KAWUNIWUNI WA CHIPANGANO CHAKALE (Old Testament)

Kodi Baibulo lonse limalumikizana bwanji? Baibulo limanena chimodzi ndipo ndi buku limodzi kuchokera ku Genesis kufikira ku Chivumbulutso. Yesu ndi mutu wa Baibulo lonse.

Kotero chinthu chimodzi cholumikidzanachi m'Baibulo ndi cholembedwa ndi Mulungu. Mau onse a m'Baibulo ndi mau a Mulungu. M'Baibulo muli zinthu zomwe Mulungu amafuna kuti ife timudziwe. Mau ena aliwonse, adalembedwa ndi chilangidzo chathu, Aroma 15:4 pakuti zonse zinalembedwa kale zinalembedwa kutilangiza, kuti mwa chipiriro ndi chitonthozo cha Malembo, tikhale ndi chiyembekezo.

Baibulo limalongosola bwino kuti Mulungu ali ndi dongosolo limodzi, muzonse zomwe zili mumbiri.

Ali ndi cholinga—dongosolo la kukwaniritsidwa kwa nthawi, kulumikidza zinthu zonse mwa Iye (Khristu), zinthu za pansi pano ndi zinthu za kumwamba.

Ali ndi cholinga pakuchita zimenezi—Aefeso 1:12 akuti "kuti ife amene tinakhulupirira Khristu tikayamikitse ulemerero wake. Mulungu adatilenga ife chifukwa cha ulemerero wake."

Dongotsolo limeneli wakhala ali nalo nthawi zonse Yesaya 46:9-10, kumbukirani zinthu zoyamba zakale, kuti Ine ndine Mulungu, ndipo palibenso wina; Ine ndine Yehova ndipo palibenso wina wofana ndi Ine; ndilalikira za chimalidziro kuyambira pa chiyambi, ndikuyambira nthawi zakale ndinena zinthu zomwe sidzinachitidwe; ndi kunena Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzachita zofuna zanga zonse.

Dongotsololi lili mu nthawi zake Agalatiya 4:4-5 koma pokwaniridwa nthawi, Mulungu anatuma Mwana wake, wobadwa ndi mkazi, wobadwa wakunvera lamulo, kuti akaombole iwo akunvera lamulo, kuti ife tikalandire umwana.

Ntchito ya Khristu padziko lapansi ndi chinthu chofunikira kwambiri mumbiri. Timatembenuka m'mbuyo ndikuyang'ana mtanda, komanso ntsogolo ndikuyang'na kubweranso kachiwiri kwa Khristu kukamalidza ntchito yake. 2Petro 3:13 koma monga mwa lonjezano lake tiyembekedzera miyamba yatsopano, ndi dziko latsopano m'menemo mukhalitsa chilungamo.

Umodzi wa dongotsolo la Mulungu, zimapangitsa Iye kulotsera za zinthu zochitika ntsogolo ndiponso malonjezowa kuti akwaniritsidwe monga kubwera kwa Mesiya (Yesaya 9:6-7).

Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wa mwamuna wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala paphewa lache, ndipo adzamutcha dzina lache, Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wantendere. Za kuyenjedzera ulamuliro wache, ndi za mtendere sidzidzatha pa mpando wachifumu wa Davide, kuukhadzikitsa ndi kuuchirikidza ndi chiwerudzo ndi chilungamo kuyambira tsopano ndikunkabe nthawi zonse. Changu cha YEHOVA wa makamu chidzachita zimenezi.

Pali ulosi umodzi wansogolo umene uli kubwera, onani 2Petro 3:13 vesi yomwe ili pamwambapa. Pokhala kuti pulani ya Mulungu imanena za Khristu ndi ulemerero wake, ndichachidziwikire kuti mfundo zonse za Chipangano Chakale zimalodza kwa Yesu 2Akolinto 1:20 “Pakuti monga mawerengedwe a malonjezano a Mulungu ali mwa Iye eya; chifukwa chakenso ali mwa Iye amen, kwa ulemerero wa Mulungu mwa ife.

Yesu adataya nthawi pakuphunzitsa kuti Chipangano Chakale chimalodzera kubwera kwa Iye. Luka 24:44 “ndipo adati kwa iwo, Awa ndimauwo ndinayankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwanitsidwa zonse zolembedwa za Ine m’chilamulo cha Mose ndi aneneri, ndi Masalmo.”

Luka 24:45-48 ndipo anawatsegulira mitima yao, kuti adziwitse Malembo; ndipo anati kwa iwo “kotero kwalembedwa, kuti Khristu anve zowawa, nauke kwa akufa tsiku la chitatu; ndi kuti kulalikidwe m’dzina lache kulapa ndi kukhululukidwa kwa machimo kwa mitundu yonse, kuyambira ku Yerusalemu.

Inu ndi mboni za izi

Iye Mulungu anawatsegulira mitima yao, kuti adziwe malembo Luka 24:45. Chipangano Chakale chimayang’ana za kukwaniritsidwa kwa chipulumutso zomwe zidachitika kamodzi m’moyo mu imfa ndi mkuuka kwa Yesu Khristu.

Malonjezo a Mulungu

Kodi Chipangano Chakale chimayang’ana bwanja kubwera kwa Yesu Khristu? Pali malonjezo a padera mu Chipangano Chakale amene mwachindunji a amalodza ku kubwera kwa Yesu Khristu ngati Mesiya. (Mika 5:2,Yesaya 7:13-14 ndi 9:6-7 ndi 40:3-4 ndi 53:1-4 ndi Masalmo 45:6-7 ndi Masalmo 22:1-21 ndi Masalmo 2:7 ndi Masalmo 78:1-2, Yeremiya 31:15, Hoseya 11:1, Zekariya 9:19. Baibulo lonse limatilodzera kwa Yesu Khristu. Chipangano Chakale chmalodzera kutsogolo pamene Chipangano Chatsopano chimatilodzera kwa Yesu anadza m’mbuyomo.

Zolembedwa zotsatiladzi, zikunena za mabuku onse a Chipangano Chakale, amene zikhale zipangizo panthawi ya makalasi. Ndikwabwino kuphunzitsa za aneneri angapo kenako kupitilidza ndi Chipangano Chatsopano. Komabe ndikwabwino kuti pakutha pakugawa masatifiketi kwa omalidza maphunzirowa, kalasi ipitiridze kuphunzirira pamodzi ndi kukambirana ndikumalidza kuona za aneneri onse ndi kuphunzira modzama mabuku ena onse a mu Baibulo.

Kwazaka 2500 nkhani ya Mulungu yakhala ikukambidwa kawirikawiri monveka bwino kumibado yonse kufikira lero. Iyi idali njira yodalilika yotsungira mbiri ndipo njirayi ikupitirira m’madera ambiri momwe anthu satha kulemba chiyankhulo chawo. Mabuku asanu oyambirira M’baibulo adalembedwa ndi Mose. Ali mu gawo la Chipangano Chakale omwe amadziwika ndi dzina loti Pentanchu (mabuku asanu) kapena tora (lamulo)

Genesis akunena momwe Mulungu, adalengera china chilichonse kuti chidali bwino chifukwa tchimo kudalibe. Potsakhalitsa Adamu ndi Hava adachimwa ndipo mavuto onse a padzikoli adadza kuchokera ku tchimo loyamba. Pambuyo pa tchimo loyambali, munthu sadatsiye kuchimwa zomwe zidapangitsa Mulungu kubweretsa chilango kwa munthu. Tikuphunzira kuti Mulungu amalanga tchimo ndi chilango choopsa zedi. Tikuphunziranso kuti munthu atangochimwa nthawi yomweyo Mulungu adayamba

kukonza ndondomeko yopulumutsira munthuyu mu uchimo ndikubwedzweretsa ubale wa bwino ndi munthu. Mulungu akulengedza pa Genesis 12 kuti achita pulani yake ya chipulumutso kupyorera mwa Abramu (Abrahamu) ndi kwa Mbeu zake kuphatikidzapo Yesu.

I.Chiyambi cha nthawi mu Genesis mutu 1-11 akunena za zaka 2000 zoyambirira. Muli zochitikachitika zinayi mu mitu 11 imeneyi.

1.Choyamba ndi zokhudzana ndi chilengedwe. Genesis 1:1-2. Ndizofunikira kwambiri kuti tinvetsetse za nkhani ya kulengedwa kwa zinthu-Chifukwa chiyani? Dziko likuphunzitsa za Evolution, limeneli ndi ganizo lomwe limakana kuti zinthu zonse zidalengedwa ndi Mulungu, koma kuti zinthu zidangopedzekako mwa izo zokha. Izi ndizolakwika kwambiri. Baibulo limanena kuti Mulungu adayankhula ndipo adalenga chilichonse kuchokera kopanda kanthu, zomwe ndizoona. Yohane 1:3 akutiudza ife kuti palibe chidalengedwa popanda Yesu. Iye ndiye Mlengi wathu, ndipo amatsunga chilichonse kuti chidzigwira ntchito yake.

A. werengani 1-13. Tinvetsetse kuti kudali kotsavuto kwa Mulungu kulenga dziko lonseli ndi zonse zamoyo. Izi zitithandidza kunvetsetsa kuti Mulungu wathu ndi wamphmvu komanso alibe malire. Tiyime kutali ndi Iye; ndipo tiyenera kumupatsa ulemu waukuru. Zomwe adalenga zimaulula za momwe Iye alili. Mwachitsanzo, tikudziwa kuti amakonda kukongola komanso mitundu.

B. Genesis 1:27 munthu adalengedwa muchifanidzilo cha Mulungu. zikutanthaudza chiyani?zikutanthaudza kuti tili ndi umunthu ofanana ndi Mulungu- tili ndi chidziwitso, kukhudzika ndi chifuniro, komansi kuthekera kosankha chabwino kapena choipa-kulingalira. Tili ndi khalidwe lotidzindikiritsa zabwino pakati pa zoipa komanso tili ndi uzimu omwe umatilola kukhala muubale ndi Mulungu. Nyama zonse zimaziyang'anira zokha.

C. Genesis 1:26-30 Mulungu akumuudza adamu kuti alamulire dziko lapansi. 1Akolinto 6:2-3 akuti Oyera adzawerudza dziko lapansi. Sindife nyama chabe, koma ndife olamula chifukwa tili ndi ubale wapaderadera ndi Mulungu.

D. Mfunso lomwe limafunsidwa kawirikawiri ku Uganda ndilakuti, ngati kulera ndikolakwika kutengera pa Genesis 1:28. Ngakhali ili lili mfunso lofunika pakati pa anthu a ku Africa, silimaoneka kukhala lofunika ku maiko a ku ulaya/azungu. Ndikunena izi chifukwa cha ndemanga zomwe ndakhala ndikudziwerenga zokhudzana ndi ndimeyi zomwe sidzinena za kudzadza dziko lapansi. M'malo mwake amakokomedza za udindo omwe anthu tili nawo wolamulira dziko lapansi.

Ndikuganidza kuti tiyenera kumatsulira ndimeyi yonseyi kuchokera pa vesi 26 kulekedzera vesi 31. Ndimenyi ikuonetsa kuti ikutiphunzitsa zakuti ife anthu tidalengedwa mopatulika kwambiri; muchifanidziro cha Mulungu. Pachifukwa ichi, tapatsidwa udindo olamulira dziko lapansi. Titha kutaya nthawi yambiri tikulingalira za ndime imeneyi, koma ine ndadzipatsa malire ndekha kunfunsoli maka pa mfundo yakuti kudzadza dziko lapansi.

Panthawi imene lamuloli limaperekedwa, padali anthu awiri okha padziko lonseli, ndipo mwachidziwikire, dzikoli limafunikira kulidzadza ndi anthu ndicholinga choti

anthuwo alilamulire. Kodi lero pali anthu okwanira kulamulira dziko lapansi? Ndiloleni ndigawane nanu maganizo anga motere pankhaniyi. Ine ndikuti ife anthu takwaniritsa lamulo lakudzadza dziko lapansi ndipo kuti kulera sitchimo chifukwa tsopano pali anthu okwanira kulamulira dziko lapansi.

Zotsatira zili munsimu ndi mfundo zomwe zandipangitsa kuyankhula motere:

1. Chiwerengero cha anthu padziko lonse chakwera kuchokera pa anthu awiri aja kufika pa anthu 7,000,000,000.
2. Lero, padziko lapansi pali anthu opotsa oyenera kulamulira dziko lapansi. Tili ndi maumboni pa ganizo ili pakungoona momwe munthu wapangira nyama kutha kapena kutheratu. Mbali zambiri za dziko lapansi zaonongedwa chifukwa cha zochita za munthu monga kuononga kwamitengo zomwe zikupangitsa mavuto a kukokololoka kwa nthaka.
3. Mbali zochuluka za pa dziko lapansi zikuvutika ndi njala komanso chilala chifukwa, anthu achuluka ndipo chakudya chikuchepa m'madera aterewa.

Ngakhale sikoyenera kwa ine kunena kuti kodi ndi ana angati amene munthu angabereke, ndinganene kuti, potengera 1Timoteo 5:8 Mulungu akufuna inu kukhala ndi ana omwe mungakwanitse kuwatsamalira. Amene mungakwanitse wadyetsa bwino, kukhala ndi malo okhala, kuwapatsa zovala, chitsamaliro cha chipatala, nthawi yochedza ndi makolo, komanso kukwanitsa kuwapatsa maphunziro kwa ana onse omwe mungabereke.

Mabanja ambiri kwa azungu amangokhala ndi ana awiri okha. Pali zifukwa zake zomwe amachitira izi monga:

1. Mudziko lao alimo anthu okwanira.
2. Kulera ana ndikodula kutsiyana ndi kuno kwathu, mayiko a kwa azungu amaudza makolo kulipira ana awo kuboma. Sungawatsiye anawa mwachitsawawa. Kulephera kulipira anawa kapena kuwapatsa chithandidzo ku dziko la United States ku America zotsatira zake ndi kumangidwa kwa makolo.

3. Khalidwe lachikhristu ndilakuti makolo ayenera kutsamalira ana awo.

Njira ya kulera imene imaletsa mbeu ya Abambo kuti itsakumane ndi mbeu ya a mai siyolakwika kapena tinene kuti kugwiritsa ntchito njira imeneyo sitchimo ayi. Koma njira yomwe imapha mwana amene wayambika kale m'mimba ndiyolakwika ndipo kumeneko ndikupalamula mlandu wakupha. Mankhwala amakono akupedzeka ogwiritsa ntchito pofuna kutsata njira zolera.

E. Genesis 1:31 zolengedwa zonse zidali bwino. Chifukwa chiyani? chifukwa tchimo kudalibe monga momwe kudalili kumwamba.

F. Genesis 2:1-3 Mulungu adakhadzikitsa tsiku la chitsanu ndi chiwiri ngati lopatulika kuti likhali lopumulira. Ndikofunikira ngakhale lero kutsamalira tsiku la Sabata.

i. pakufunika tsiku limodzi lopuma lomwe tingakapembedzere Mulungu.

ii. Anthu amafunika tsiku limodzi pasabata kuti apume kuntchito zao. Mulungu adakonza kuti ife anthu tidzifuna tsiku limodzi kuti tidzipuma ndi kumasuka komansi kuchedza ndi banja lathu. Timagwira ntchito bwino tikakhala kuti tsiku limodzi sitikugwira ntchito pasabata, ndipo ntchito zimayenda bwino pamene tazigwira kwa

matsiku asanu ndi limodzi pasabata kutsiyana pamene tagwira ntchito matsiku onse a musabata.

G. Genesis 2:4-25 Mulungu akubweredza nkhani ya chilengedwe kuyankhula zambiri za anthu amene ali opambana kupotsa zolengedwa zonse. Akutiudza ife zambiri zokhudzana ndi chiyambi chathu. Iyi sinkhani yachilengedwe yotsiyana ndi yomwe taiona kale, koma monga ndanena, iyi imamulola Mulungu kukamba za zolengedwa zopotsa muchilengedwe yemwe ali munthu.

i. Genesis 2:15-17 akutiudza ife kuti tili pantchito. Kodi tidzagwiranso ntchito kumwamba?

ii. Chaputala 2:18-24 akutipatsa satanesatane wokhudzana ndi ubale womwe mkazi ndi mwamuna ali nawo kupyorera mukulengedwa kwa Hava. Vesi 18 ikutiphunzitsa kuti mkazi adalengedwa kuti akhale othangatira mwamuna ndipo vesi 24 ikutipatsa ife madziko a banja la chikhristu lomwe ndi munthu m'modzi mwa awiriwo ndipo pakuti sitingadzipange nkhaza tokha, koteronso sitidzachita nkhaza akazi athu.

iii. Ndiponso sitidzalekene chifukwa pamene takwatirana timakhala munthu m'modzi ndipo zoona zake sitingagawanikane. Mulungu amadana ndi kulekana pa ukwati.

2. Chochitika chachiwiri mu mitu 11 yoyambirira ndi kugwa kwa munthu

A. Gen. 3:1-7 tchimo lilowa padziko. Munthu adali ndi ufulu wa chifuniro chake kutsankha kunvera Mulungu, kapena kutsanvera Iye, ndipo Adamu adatsankha kutsanvera Mulungu ndipo ili lidali tchimo loyamba. Ndipo munthu wakhala akutsankha kutsanvera Mulungu. Mavuto onse ali padzikoli adabwera chifukwa cha tchimo longochitika kamodzi kokha. Aroma 3:23 ndi Aroma 6:23.

B. motsachedwetsa Mulungu adapereka chilango kwa njoka, Adamu, Hava ndi chilengedwe chonse. Genesis 3:14-19, Aroma 8:19-23 moyo ukudzunzika chifukwa cha tchimo loyambali. Tchimo ndi vuto lalikulu kwambiri ndipo Mulungu amapereka chilango kumachimo onsewa. Munthu amalandira zilango za mitundu iwiri:

i. chilango chapansi pompano chomwe chimaperekedwa kwa Akhristu kapena ayi. Chitsanzo ndichakuti munthu aliyense amene achita chigololo ndi munthu yemwe ali ndi nthenda ya EDZI munthuyunso atha kutenga Edzi kudwala nayo mpaka ndikufa.

ii. Chilango chotsatha

a. Munthu otsapulumutsidwa amapita kugahena pamene wamwalira ndipo adzavutika kumeneko kwamuyaya chifukwa cha machimo ake.

b. Mkhristu chilango chake chidalandilidwa kale ndi Yesu, ndipo iye adzapita kumwamba. Yesu adalangidwa pamtanda chifukwa cha machimo amene adzachite ndi mkhristu wina aliyense.

C. Genesis 3:8-15 mulungu amafunafuna munthu ndikukudza chisomo potsachotsa moyo wamunthu nthawi yomwe adangochimwayo. Mulungu adayamba pulani yake ya chiyanjano.

i. muvesi 8 ndi 9 mulungu akuyamba dongotsolo lachiombolo kapena lopulumutsa munthu pamene ntchimo lidali litangochitika kumene. Mulungu akufunafuna munthu kuti akhadzikitse kapena kuyambanso ubale wao.

ii. Vesi 21 ikunena kuti Mulungu adapha nyama ndikupanga zovala kumpatsa Adamu ndi Hava. Kupha kwa nyama ndi kuvekedwa kwa Adamu komanso Hava zimaonetsa kuti:

a. Munthu akuyenera kuvekedwa kuti ayime pamaso pa Mulungu Oyera.

b. Munthu payekha ndi ntchito zake sangathe kudziveka yekha ndikudziyeneredza yekha kukhala ovomeredzeka pamaso pa Mulungu. Zimatengera ntchito ya Mulungu kuti munthu akhale ovomeredzeka pamaso pa Mulungu.

c. Mulungu adzapereka chomwe chili chovomeredzeka pamaso pake.

d. Mulungu adapha nyama zotsachimwa kuonetsa kuti kukhetsedwa kwa mwazi ndikofunikira kuti munthu apedzenso Paradaizo. Mchitidwe okhetsa mwazi wa nyama zolungama zimalodzera kubwera kwa msembe yangwiro ya Yesu Khristu pamene mwazi wake udakhetsedwa.

iii. Mulungu adapanga pangano logonjetsa Satana mu Gen. 3:15 vesi yofunikira kwambiri chifukwa ndi amene akuneneratu za kugonjetsedwa kwa Satana ndikupambana kwa Yesu Khristu.

a. Kulalira chitende zikutanthaudza kuti Satana adzamuvuladza Yesu zomwe zidachitika pantanda. Pantanda Yesu adazunzika chifukwa cha tchimo lililonse lomwe mkhristu adzalichite.

b. Kulalira mutu zikutanthaudza kuti Yesu adzamupha Satana ndipo padali pantanda pamene Yesu adagonjetsa Satana, Yesu adapambana nkhondoyo.

3. Genesis 4 akuyankhula za Kaini ndi Abele ngati anthu oyamba kubadwa mwa chilengedwe cha munthu. Tikuona kuti Kaini adapha Mbale wake. Khalidwe la uchimo likuyenda kuchoka mwa Adamu kupita kumtundu onse wa anthu. Anthu akupitilidzabe kuchimwa, ndipo tikamayang'anabe Baibulo, tikuona kuti munthu akumangochimwirachimwirabe ndipo Mulungu adzalanga tchimo lililonse. Pachifukwa ichi munthu akufunikira mpulumutsi.

4. Chochitika chachikulu chachitatu mu mitu 11 ya Genesis, ndi chigumula. Genesis mutu 6-9 akunena za nkhani ya Nowa ndi chigumula.

A. Tchimo likupita ndilikukulirakulirabe, padziko lapansi ndipo Mulungu akunena zakulanga ntundu onse wa anthu. Genesis 6:5-7 Mulungu akunena za momwe adanvera chisoni chifukwa cha tchimo la munthu.

B. Tikuona muvesi 8 kuti Nowa yekha adapedza ufulu pamaso pa Mulungu. Kuyambira pa vesi 13-14 Mulungu akuyankhula ndi Nowa kuti aseme chingalawa kotero kuti Iye ndi banja lake adzabitsalemo nadzapulumuka ku chigumula chobwera patsogolo pao pamene mtundu onse wa anthu udzaonongeke.

C. Nkhani ya chigumula chachikuru imatiudza kuti tchimo likunka ndilikula, kufikira pamene Mulungu akuonetsa nkwiyo wake pa tchimo, pakutumidza chigumula ngati chiweruzo choopsa zedi. Tikuona kuti Mulungu amalekerera anthu, koma pamene kulekerera kwake kwafika potsalapika, amabweretsa chiweruzo choopsa kwambiri.

i. Genesis 6:22 akunena kuti Nowa adanvera Mulungu. Ahebri 11:17 akutiudza kuti Nowa adapulumutsidwa ndi chikhulupiriro monga zimakhalira ndi mkhristu wina aliyense. Kupyorera mu chikhulupiriro cha mwa Yesu Khristu.

5. Chochitika chachikulu cha chinayi mumitu ya Gen 1-11, ndi zokhudzana ndi sanja ya Babulo. Munthu akuchimwira chimwirabe.

A. Genesis 11 ndi nkhani ya sanja la Babulo. Anthu akudza pamodzi kuti atsusane ndi Mulungu. Adamanga sanja chifukwa cha kunyada kwao kwakukuru komanso chifukwa cha kusanvera zoikika za Mulungu zomwe zili mu Genesis 9:1 kuti adzadze dziko lonse lapansi.

B. Potsagwiridzana ndi zimenezi, chomwe Mulungu adachita ndi kutsokonedza zilankhulo zao kuti asanvane wina ndi nzache zomwe mapeto ake adali kumwazikana kwa ntundu wa anthupadziko lonse lapansi.

II. Gawo lina la bukuli kuyambira mutu 12 tikunva nkhani za anthu okwana anayi omwe adagwiritsidwa ntchito kopambana ndi Mulungu. Anthuwa ndi Abrahamu, Isaki, Yakobo, ndi Yosefe, amenewanso amatchedwa makolo a Ayuda.

1. Woyamba mwa anayiwa ndi Abram amene zina lake linasandulika kukhala Abrahamu. (Abrahamu amatchulidwa kuti Abramu kufikira kubadwa kwa mwana wake Isaki). Iye ndi tate wa mtundu wa Ahebri; tate wa Ayuda

A. Gen. 12:1-4 akuitanidwira ku dziko loyera—kodi Abramu adaitanidwa chifukwa adali munthu wangwiro? Ayi adali wachikunja ndi wamantha—adamupereka kawiri konse mkazi wake pofuna kupulumutsa moyo wake. Umu ndimomwe Mulungu amawafikira anthu ochimwa. Komabe tikuwerenga apa kuti ndi chikhulupiriro Abramu adachoka kwao natsatira Mulungu, ndipo Abrahamu amadziwika kuti ndi munthu wachikhulupiriro chodzama, onani Ahebri 11:8-19

i.Gen. 12:1-3 Mulungu akulowa mpangano ndi Abramu. Awa ndi mavesi akuruakuru afunikira kulowedza. Ili limadziwika kuti ndi pangano pangano la Abrahamu pamene Mulungu akuwulula m'mene adzagwirire ntchito kuti abwedzeretsenso ubale wa mtendere ndi munthu. Adzachita pulani yake ya chipulumutso kudzera mwa Abrahamu ndi Mbeu zake. Yesu ndi Mbewu ya Abrahamu. Akupatula anthu odziwika ndi dzina lokuti Ahebri, kapena a Israeli, kapena kuti Ayuda ngati anthu enieni a Mulungu amene adzagwire nawo ntchito.

B.Gen. 15:1-21 Mulungu akuyika chidzindikiro papanganoli omwe uli mwazi. Izi zikupangitsa panganoli kukhala lopambana. Mapangano ali ngati m'gwirizano, pakati pa Mulungu ndi munthu. Mapangano ambiri ndi malonjezo kuchokera kwa Mulungu ndipo munthu safunikira kuchitapo china chili chonse, monga momwe lilili panganoli. Komabe mapangano ena monga pangano la m'dulidwe munthu amayenera kuchitapo china chake, onani chaputala cha 17 kuti muphunzire zambiri za pangano la m'dulidwe.

i.Gen.15:4 Abramu adalonjedzedwa mwana koma ngakhale Abramu ndi munthu wa chikhulupiriro chodzama mwa Mulungu, nthawi zina amakayikira kuti zomwe Mulungu amanena zingatheke. Abramu amaganidza kuti iye ndi mkazi wake ndi okalamba kwambiri. Tikuphunzira kuti nthawi zina chikhulupiriro chathu chimafooka, koma kenako chimakulanso. Izi zimachitika kwa ife tonse.

C.Gen. 16 ndi nkhani yonena za kutsakhulupirira kwa Abramu ndi mkazi wake pamene anatenga wantchito wa mkazi wake ndikumuberekera mwana wamwamuna namutcha dzina lake Isimaeli. Ngakhale Ahebri 11:8 akunena kuti Abrahamu adali munthu wa chikhulupiriro; koma tikuona kuti chikhulupiriro chake chimafoka monga amachitira wina aliyense. Mwana wa Abrahamu Ismaeli adabadwa ndipo iye ndi kholo la Aluya omwe adabukitsa chipembezo cha chisilamu, amenenso pakadali pano ndi adani a Israeli. Kutsakhulupiriraku kudabweretsa adani oipa a Israeli kuti akhaleko.

D.Gen.17 akufotokoza zokhudzana ndi pangano la m'dulidwe. Vesi 1-6 lili ndi lonjezo kuchokera kwa Mulungu, kuti pa nsinkhu wa zaka 99 Abramu adzatchedwa ndi

dzina lina loti Abrahamu chifukwa walonjezedwa za mwana wa mwamuna wolandira cholowa ndipo malingana ndi lonjezo la Mulungu pambuyopo iye adzakhala tate wa makamu.

i. Mulungu adalonjeza madalitso kwa Abrahamu ndi kwa mbeu zake. Lonjezoli ndi Yesu komanso chipulumutso chathu kudzera mwa Iye.

ii. Mu vesi 9-14 tili ndi pangano la m'dulidwe momwe Ayuda akupatulidwa ngati ntundu wa anthu opatulika wa Mulungu. M'dulidwe ndi chidzindikiro chomwe chimapatula ana a Mulungu pamaso pa ena onse monga momwe ulili ubatizo matsiku ano kwa akhristu. Ili ndi phunzironso mu chipangano chakale kuti ife akhristu tikukhala padziko lapansi koma si ife adziko lapansi. Kwathu kwenikweni ndi kumwamba komwe kuli Mulungu wathu. Onani Yohane 17:14-16 ndi 18:36.

iii. Mu vesi 15-19 Mulungu akulonjeza kudalitsa Sarai ndi mwana, ngakhale ali ndi zaka 90, ndipo dzina lake lidzasintha kukhala Sara, lomwe ndidzina loyenera lomwe likutanthudza kuti mfumu kazi chifukwa Iye ndi mayi wa mafumu.

iv. Kachiwiri, mu Genesis 17:17 tikuona kusowa kwa chikhulupiriro mwa Abrahamu, pamene akukayika kuti Sara adzakhala nakubala. Ndipo mwana wake adzatchedwa Isaki kutanthaudza kuti "mwana wa lonjezo" ndipo akubadwa chaka chomwecho.

E. Genesis 18-19 pali nkhani ya Sodomu ndi Gomora—nkhani yoopsa yomwe munthu woipa amakhalira ndi momwe kuopsa kwa chiweruzo cha Mulungu chimakhalilanso.

i. Gen. 18:1-15 akunena za alendo a kumwamba. Tikuona mu vesi 3 kuti Abrahamu akudzindikira kuti Mulungu wabwera kumuchedzera. Abrahamu akulandira bwino alendowa, ndipo akutsimikidzilidwa kuti akhala ndi mwana chaka chikubweracho. Ndiye tikuona kuti Sarai, adanva zonenedwazo ndipo ndi kutsakhulupirira adayamba kutseka. Onani kuyankha kwa Mulungu mu vesi 14 pamene akufunsa "kodi chilipo chinthu chomlaka Yehova?" werengani Luka 1:34-38 kuti muone momwe funsoli akuliyankhira.

ii. Nkhani ya Sodomu ndi Gomora ukubwera pambuyo pake. Genesis 18:20 mulungu akuulura kutsakondwa kwake motsutsana ndi anthu aku Sodomu ndi Gomora chifukwa cha kuipa kwao monga momwe adaonetsera kutsakondwa kwake ndi ntundu wa anthu munthawi ya Nowa. Vesi 21 Mulungu akunena kuti anthu amenewa akuyenera chionongeko. Machimo awo ndi ambiri, amapanga za umathanyula zomwe zimakwiyitsa Mulungu koopsa. Tchimoli ndi kuononga mphaso ya banja yomwe Mulungu adatipatsa.

a. vesi 22-33 akuonena momwe adamu adapembedzera Mulungu. Tikuphunzira apa kuti nthawi zina ndi bwino kupembedzera Mulungu bola ngati izi tikudzichita moyenerera ndipo chidandaula chathu ndichifukwa chonveka. Onaninso kuti kupembedzera kwa Abrahamu sikudali kuti kupindulire iye mwini; koma kudali kutetedza anthu otsachimwa opedzeka mu Sodomu ndi Gomora. Kupembedzera kwa Abrahamu kudali kochokera pa chilungamo cha Mulungu ndipo izi ndizomwe adapempha.

b. Gen. 19 akunena momwe Mulungu adaonongera mizinda iwiriyi chifukwa cha tchimo lonyasa la anthu; ndikupulumutsa Loti pamodzi ndi banja lake. Timawerenga kuti chilangochi chidali chachikuru pamene sufule ndi moto zidaononga mizindayi. Genesis 19:24.

c. tikuonabe kuti ngakhale adalanditsidwa, Loti ndi banja lake adalangidwanso chifukwa chotsanvera. Adalangidzidwa kuti pamene akuthawa atsatembenuka

ndikuyang'ana m'mbuyo, mkazi wa Loti sadanvere ndipo nthawi yomweyo adatsanduka chulu cha nchere. Genesis 19:17 ndi 26

d. Genesis 19:30-38 akunena za nkhani ya manyazi yokhudzana ndi Loti pamodzi ndi ana ake a akazi. Ndi nkhani yakutsakhulupirira kwa ana a Lotiwa pamene anamwetsa atate wao mowa ndicholinga kuti agone nawo kuti akhale ndi ana. Onse adakhaka ndi ana omwe adali atate a maiko awiri; Moabu ndi Amoni. Maiko awiriwa adali adani a Ayuda.

F. Gen. 20 ndi nkhani yonena za kupambana kwa pemphero pamaso pa Mulungu. Tikuwerenga kuti Abrahamu pofuna kutetedza moyo wake, adapereka mkazi wake kwa Abimeleki. Komabe, Abimeleki asadakhale ndi Mkazi wa Abrahamu Sara, Mulungu adamuchenjedza kuti afa pokhapokha ngati Abimelekiyo apempha Abrahamu kuti amupemphere. Tinganene kuti, Mulungu amafuna pemphero asadachite ndi mfumu Abimeleki pomukhululuka. Nkhaniyi ndi yaikulu kwambiri, yokhudzana ndi mphamvu za Mulungu komanso mphamvu ngakhale kufunikira kwa pemphero.

G. Gen 21 mwana wa lonjezo Isaki akubadwa. Mulungu nthawi zonse amasunga lonjezo. Kutengera Tito 1:2 Mulungu sanama.

H. Gen. 22 mulungu akulamulira zakuti Isaki aperekedwe msembe. Tikuona apa chifukwa chomwe Abrahamu amatchedwa munthu wachikhulupiriro chodzama chifukwa adanvera Mulungu ndi kukonzeka kupereka mwana wake Isaki msembe. Tikuona kuti pamapeto pake Mulungu adapereka m'malo mwa Isake nkhosa kuti iperekedwe msembe. Izi zimalodzera kubwera kwa Yesu yemwe adaperekedwa ndi Mulungu ngati nkhosa kuti ikaperekedwe msembe pantanda chifukwa cha machimo athu.

I. Gen. 24 Isaki amadziwika kwambiri kuti adali bambo wake wa Yakobo. Abrahamu adatumudza wantchito wake kupita kudziko lakwawo kuti akatenge mkazi, pakuti adati Isaki asakwatire mkazi ntundu wina. Kusogoloku tiona momwe akazi a chilendo adapangira kuti ana a Mulungu agwe m'mavuto. Abrahamu adadziwa ndi kutsatira chifuniro cha Mulungu. Tingadziwa bwanji chifuniro cha Mulungu? Werengani Baibulo ndi kupemphera kuti Mulungu akuululireni matanthaudzo odzama a m' Baibulo.

J. Mutu 25 tikuona za kumwalira kwa Abrahamu komanso kubadwa kwa mapasa, Yokobo ndi Esau ana a Isaki. Yakobo amatanthaudza onama—Yakobo adali wachiwiri kubadwa koma adanyengerera mkuru wake Esau kuti amupatse ukuru wake ngati mwana woyamba kubadwa komanso kumunyengerera kuti amupatse madalitso a mwana woyamba kubadwa omwe Esau adali nawo. Yakobo sikuti amafuna kumunyenga nkuru wakeyu koma amachita izi chifukwa Mulungu sadasankhe Esau koma adasankha iye m'malo mwa Esau Gen. 25:23 ndi Aroma 9:10-13 mulungu ndi wamphamvu zonse ndipo amasankha iwo amene adzawakonde.

2. Kholo lachiwiri ndi Isaki.

A.Gen. 26:2-4 kupangidwanso kwa lonjezo lamadalitso lomwe lidapangidwa pachiyambi ndi Abrahamu. Ichi ndi chikumbutso kuti dalitsoli ndi loyenera ndipo lidzakhalapobe. Baibulo silikunena zambiri zokhudzana ndi Isaki.

B. Isaki adakana kuti Rabeka ndi mkazi wake monga momwe Bambo wake adachitira, onani Genesis 26:7.

3. Kholo lachitatu ndi Yakobo. Tikudziwa kuti Yakobo ndi munthu wotani molingana ndi tanthaudzo la dzina lake kuti onama kapena onyenga. Adali atate wa ana 12 omwe adapanganso mitundu 12 ya ana a Israeli.

A.Gen. 28 akunena za kuthawa kwa Yakobo kupita kudziko la Padaniramu kwa malume ake a Rabani kuzemba mkwiyo wa Esau pamene anaba madalitso ake oyamba. Genesis 27:41-42 akutiudza kuti Esau amafuna kupha Yakobo. Sopano Yakobo ndi okuba komanso onama, koma amalume ake a Rabani ndi onama kupotsa Yakobo ndipo adakhala akumunamidza mowirikidza.

B. Yakobo adali yekha pamene amathawa mkwiyo wa m'chimwene wake Esau nkuthekanso kuti amachita mantha pamene amayenda m'mizinda yomwe idali ya chilendo. Genesis 28:10-19 akunena momwe Mulungu anabwerera kwa iye mu maloto ndikumulimbikitsa. Tikuona kuti ngakhale Yakobo adali yekha muchipululu, sadali yekhayekha, chifukwa Mulungu adali ndi iye. Mateyu 28:20 amatiudza kuti Mulungu alinafe nthawi zonse. Yakobo adabadwira m'banja lolemera koma pano tsopano ali yekha ndipo alibe chuma kotero Mulungu adamuonetsera chikondi chake ndi kumulimbikitsa komanso kumutonthodza.

i. Mulungu akubweredza mu Genesis 28:13-15 lonjezo lomwe adapangana ndi Abrahamu pomuudza Yakobo kuti iye ndi olowa m'malo wa lonjezoli. Adamuudza Yakobo kuti chilichonse chidzakhala bwino ndi iye ndipo akhala moyo ndipo kuti adzabwerera ku dziko lomwe Mulungu adamulonjeza Abrahamu ndi mbeu zake. Mulungu adamutsimikidzira Yakobo kuti adzakhala ndi banja.

C. Mutu 29 akukamba nkhani ya Yakobo momwe adakumanira ndi kugwa muchikondi ndi Rakelo ndipo adavomeredza kugwira ntchito kwa amalume ake zaka zokwana 7 kuti atenge Iye akhale mkazi wake. Timawerenga momwe ukwati udachitikira komanso m'mene yakobo adazindikirira kuti malume akewo adamunamidza pakuti adali Leya otsati Rakero monga momwe iye amafunirira.mukuganidza kuti izi zingatheke bwanji? Labani amafuna kuti Yakobo agwirenso ntchito kwazaka 7 kuti atengenso Rakero. Kotero Yakobo adakumana ndi zovuta chifukwa chokhala ndi akazi awiri.

D. Genesis 31:1-55 akunena za ulendo wa Yakobo obwerera kwao zitatha zaka pafupifupi 20.

i. tikuona muvesi 1-3 ndi nthawi yoti Yakobo alekane ndi amalume ake. Mulungu adagwiritsa ntchito Labani kuti Yakobo abwerere kwao.

ii. Chinthu chofunikira kwambiri chomwe chinachitika paulendo wa Yakobo m'mene amabwerera kwao chikupedzeka pa Genesis 32:22-28 pamene adakumana ndi Mulungu. Yakobo adali wamantha pamene amakumana ndi Mulungu. Adadziwa kuti akakumana ndi m'chimwene wake Esau, amene mwina akufunafunabe kumupha iye, ndipo vesi 24 imanena kuti Yakobo adatsala yekhayekha. Ndibwino munthu nthawi zambiri azikhala munyengo zomwe Yakobo anadutsamo kuti aziona kufunikira kokumana ndi Mulungu pazosowa zake. Adalimbana ndi Mulungu utsiku onse asadazipereke kwa Mulungu. uwu udali umunthu wake kukumana ndi Mulungu pamene Yakobo adakhala munthu watsopano monga m'mene amachitira mkhristu pamene wakumana ndi Mulungu ndipo amatembenuka mtima ndipo amapangidwa kukhala munthu watsopano. Tikuona dzina la Yakobo likutsintha kuchokera pa Onama kutsinthika kukhala Israeli lomwe ndidzina labwino kwamunthu yemwe ndi tate wa mitundu 12 ya ana a Israeli. Uku ndiko kubadwanso kwatsopano kwa Yakobo ngati mwana watsopano wa Mulungu.

E. Yakobo pano ndi obadwa mwatsopano ndipo akupatsidwa dzina lina Israeli kuonetsa kuti sionamanso ayi. Koma moyo wake wonse kumapeto kwake udali wotsautsika chifukwa cha zochita za ana ake. Tikuona kuti Mulungu amagwira ntchito ndi anthu ochimwa.

i. Mutu 34 akunena za kugwiririidwa kwa mwana wa Yakobo Dina ndi mwana wa mfumu wa ku Sekemu. M'nyamatayu adafunsira banja lomwe Israeli adalikana mwanzeru chifukwa anthu a Mulunguwa adayenera kupanga maukwati ndi anthu a Mulungunso. Komanso ukwati umenewu ukadatanthaudza kuti Ahebri akadathedwa ndi ufumu waukuru wa ku Sekemu. Awa akadakhala mathero a ntundu wa ana a Mulungu umene Mulungu adakonza kuugwiritsa ntchito kubweretsa chipulumutso kudziko lonse lapansi. Yakobo adagwiritsa ntchito kubwedzera kwakukuru poononga nzinda wa Sekemu ndi anthu onse.

F. Mutu 38 akunena za nkhani yoopsa ya Yuda ndi banja lake, m'modzi wa ana a Yakobo. Tikamaphunzira ndikuona kuipa kotheratu kwa Yuda tikumbukirenso kuti Yesu ndi mbeu yake. Mobweredza, tikukumbutsidwa kuti Mulungu akhodza kugwira ntchito ndi wina aliyense potsatengera kuti iye kapena banja lake ndi loyipa bwanji.

i. Mutu 38:1-5 akunena kuti Yuda adapita nakamanga ubwenzi ndi mkanani wina nakakwatira m'modzi mwa akazi a akanani, lomwe lidali tchimo.

ii. Mutu 38:5-10 tikunva nkhani yodziwika komanso yonvetsa chisoni ya Onani, mwana wa Yakobo amene sadanvere Mulungu ndipo adalangidwa ndi imfa chifukwa cha tchimoli.

iii. Kenako muvesi 11-26 ndi nkhani yonvetsa chisoni ya Tamara amene adali mpongozi wa Yuda. Pamene mwamuna wake adamwalira adali ndi maufulu ena ake. Yuda adayenera kumupatsa m'modzi mwa ana ake kuti akhale mwamuna wake, koma Yuda sadachite izi. Kotero Tamara adakonza yekha kufikira kuti adali ndi pathupi pa mpongozi wake Yuda. Yuda adafuna kupha Tamara chifukwa cha izi ngakhale kuti iye mwini ndi amene adali ochimwa. Ndi nkhani ina yomwe ikunena momwe munthu angakhalire ngakhale ali kholo la Ambuye wathu Yesu. Ndichifukwa chiyani amafuna kupha mkazi otsati mwamuna?

3. Kholo kapena tate wotsiridza ndi Yosefe yemwe adali waulemu wake. Ndiwaulemu wake chifukwa sadaphure Mbiri yoyipa m'moyo wake wonse. Adali munthu wachikhalidwe chabwino.

A. Genesis 37 akuyamba nkhani ya Yosefe ndi momwe Mulungu adakonzera njira anthu ake kukakhala ku Igupto. Yosefe adali mwana woyamba wa Rakelo, amene adali kwa zaka zambiri pamene mchemwali wake Leya adali ndi ana ambiri. Kumbukirani kuti Rakelo adali mkazi wokondedwa wa Israeli ndipo Yosefe adali mwana wokondedwa wa Israeli ndipo wina aliyense amadziwa zimenezi. Pamene nkhani yake imayamba mkuti Yosefe ali ndi zaka 17.

B. mutu 37:5-11 tikunva kuti Yosefe adaudza apabanja ake za maloto omwe adalota kuti onse azagwadira iye ndikumupatsa ulemu. Izi sizidakwiyitse banja lakeli. Malotowa pamapeto pake adatsimikidzika kukhala mau a ulosi ndipo malotowa adakwaniritsidwa.

C. Genesis 37:28 akunena kuti abale a Yosefe adamugulitsa ngati kapolo kudziko la Igoputo kudzera mwa a Ismaeli. Mulungu amafuna kukonzera njira ya ana ake kuti adzapite ku Igoputo ndi kukhala kumeneko kufikira pamene adzakhale okonzeka kulandira dziko lao lamalonjezo, ndipo iyi ndi mbali imodzi ya pulani ya Mulungu.

D. Gen. 39:1 tikunva kuti Mulungu adamudalitsa Yosefe pamene adatsogolera kuti iye akagulitsidwe kunyumba ya Potifala, wogwira ntchito olemekedzeka wa Farao,

mfumu ya mu Igoputo. Yosefe ndi okhulupirika pamaso pa Mulungu, ndipo Mulungu anamudalitsa Iye, ndichifukwa Potifala adamuika kukhala oyang'anira zonse zochitika m'nyumba mwake. Komabe, mkazi wa Potifala amamunyengerera kuti agone naye, koma pamene Yosefe adakana kuchita zomwe amafuna, mkaziyu adamunamidzira Yosefe kuti amafuna kumugwira. Pachifukwa ichi Yosefe adaponyedwa mundende momwe Mulungu adamudalitsanso naikidwa kukhala woyang'anira ndende yonse.

E. Gen. 40 akuulula cholinga chomwe Yosefe adaponyeredwa kundende. Cholinga chidali chakuti akakumane ndi opatsira chikho wa Farao amene adali mu ndende kwa nthawi yochepa. Yosefe adamatsulira maloto a woperekera chikhoyo, amene motsachedwetsa adabwedzeretsedwa kuntchito yake. Kutsogolo kwake tikuona momwe iyi idalili pulani ya Mulungu kulola ana ake kuti adze ku Igoputo.

i. M'mutu wa 40:14 Yosefe akupempha opatsira chikho wa Farao kuti akamukumbukire akatulutsidwa mundendemo. Tikuona pa vesi 23 m'mene anthu otsakhulupirika amakhalarira monga opatsira chikho wa Farao amene adamuiwala Yosefe.

F. Genesis 41 akunena kuti patatha zaka ziwiri, Farao adalota maloto omwe padalibe amene adakwanitsa kuwamatsulira. Sopano opatsira chikho wa Farao adakumbukira kuti Yosefe atha kumatsulira malotowo, kotero adamuudza Farao amene adamatsula Yosefe kuchokera mundende kuti akamatsulire maloto ake.

i. Genesis 41:17-24 Farao akumuudza Yosefe maloto ake.

ii. Mu vesi 25-36 mulungu akupatsidwa ulemu pamene Yosefe adamatsulira maloto a Farao, ndikulotsera njala yobwera kutsogolo ndi kupereka pulani kwa mfumu yopherera njalayo imenenso idzapange Farao kukhala olemera.

iii. Vesi 37-41 kenako Yosefe adaikidwa kukhala olamulira wachiwiri wamphamvu mudziko la Igoputo. Pakadali pano ali ndi mphamvu yopulumutsa banja lake.

G. Genesis 42 njala ikukakamidza abale a Yosefe kupita ku Igoputo kukapedza chakudya, ndipo pamapeto pake Yosefe adadziulula yekha kwa abale akewo ndipo banja lakwawo lonse lidatsamukira ku Igoputo. Izi zikukwaniritsa mbali imodzi ya ulosi wakuchiyambi Genesis 15:13-14.

H. Gen. 50 Yakobo atamwalira, abale a Yosefe adayamba kuda nkhawa kuti Yosefe angabwedzere zomwe iwo adamuchita, koma muvesi 4-21 Yosefe akuulula mtima wake woopa Mulungu kwa abale ake ndikuwatsimikidzira iwo za tsogolo lawo.

i. vesi 20 ndi vesi yaikuru kwambiri; imayendera limodzi ndi vesi ya Aroma 8:28. Mavesiwa ndi zitonthozo zazikuru pamene anthu akutichitira zoipa.

I. Gen. 50:25 Yosefe akuulura khumbo lake kuti mafupa ake akaikidwe ku dziko la malonjezo.

J. Buku la Genesis likutsilidza ndi ana a Israeli ali ku Igoputo komwe Mulungu adafuna kuti akhaleko. Sikuti akungokhala ku Igoputo, komanso Mulungu adapanga kuti anthuwa adzikhala kumeneku motsangalala.

CHIDULE CHA BUKU LA GENESIS

Genesis—dziko likuyamba ndipo ndilangwiro. Munthu akuchimwa ndipo choipa chili mudziko lapansi. Pamene munthu wangoyamba kuchimwa safuna kulekedza. Tikuona kawirikawiri kuti Mulungu ndi Mulungu oweruza ndipo adzalanga tchimo. Tikuona zilango zoopsa nthawi zina kwa munthu monga Onani omwe akulangidwa komanso nthawi ina chilango chinabwera kwa munthu aliyense padziko lapansi kupatula banja la Nowa.

Litangochitika tchimo loyamba Mulungu nthawi yomweyo adayamba ndondomeko ya chiyanjano kudzera mwa Yesu ndipo tikuona pulani yake ikutambasuka. Akutsankha Israeli ngati anthu omwe amafuna kuwagwiritsa ntchito kuti akathandidzire kubweretsa chipulumutso kwa anthu onse. Ngakhale buku loyamba la Baibulo tikuona kuti Mulungu ali ndi pulani yotiombola. Tikuonanso kuti munthu mwachilengedwe ndi ochimwa ndipo sangathe kuziyanjanitsa yekha ndi Mulungu. Chipangano chonse chakale, chikupitilidza nkhani ya momwe Mulungu adakonzera chili chonse kuti panthawi yoikika, dziko likhale lokonzeka pakuoneka Yesu.

ZOMWE EKSODO AKUNENA

Bukuli lili ndi magawo awiri. Gawo loyamba, mutu 1-18, ndi nkhani ya momwe Mulungu adagwiritsira ntchito Mose kutulutsa Ahebri mu ukapolo m'dziko la Igoputo; nkhaniyi ikulodzera za Yesu yemwe adatiombola mu ukapolo watchimo. Gawo lachiwiri, likupedzeka m'mutu wa 19-40 yomwe ndi nkhani yokhudzana ndi momwe Mulungu adaphunzitsira anthu ake otsankhidwa pa Phiri la Sinai momwe angakhalire motsiyana ndi anthu ena, komanso kukhala monga anthu a Mulungu. Anthu a Mulungu nthawiyo ngakhalenso pano akuyenera kukhala otsiyana ndi anthu onse. Eksodo ndi buku lomwe Mulungu adapereka Malamulo khumi ndikuyamba kuphunzitsa anthu ake momwe moyenera angamupembedzere Iye.

Mose ndi m'modzi mwa anthu oziwika m'baibulo. Mose adali m'neneri. Adalemba mabuku oyambirira a m'Baibulo kuphatikidzapo Msalmo 90. Adali mulevi zomwe zikutanthudza kuti adali ochokera m'banja la amsembe. Zaka zake zidali 120. Deuteronomo 34:7 adayenda chifupi ndi Mulungu kwazaka zokwana 40 koma tchimo lake lidapangitsa kuti alangidwe potsakalowa mudziko la lonjezo. Mose adali munthu wodalilika wa Mulungu, koma amachita zambiri zolakwika monga kupsa mtima, komanso adali okupha. Mose adali ochimwa monga wina aliyense.

Eksodo adayambika zaka 430 kuchokera pamene Genesis adatha. Mulungu ndi yemwe amalamulira zochitika zonse adaona kuti iyi ndi nthawi yoyenera kuti anthu apite kukasamalira malo amene Iye adalonjeza kwa Abrahamu kuti mbeu zake zizawatenge ngati awoawo. Sitikudziwa kwenikweni chifukwa chimene Ahebri adakhala zaka 400 ku Igoputo. Chifukwa chimodzi ndichakuti amafuna Mulungu kuwapatsa nthawi kuti akhadzikitse chidzindikiro chawo chakuti iwo ndi dziko. Chifukwa china chitha kukhala kuti achuluke kotero kuti akhale ambiri komanso a mphamvu kuti akagonjetse anthu okhala mudziko la malonjezo la Kanani.

Eksodo 1:1-2:10 akunena za kubadwa ndi moyo wa Mose mu umwana wake. Ahebri amakondedwa ndi Farao mu nthawi ya Yosefe, koma zinthu zinasintha mu Igoputo vesi 8-10 atsogoleri atsopano adaopa ndi kuda Ahebri. Farao adapanga moyo wa Ahebri kukhala ovuta kwambiri. Udali ovuta kuti mpaka zidapangitsa Ahebri kulakalaka kuchoka mu Igoputo ndi kupita kwao. Mulungu adaona kuti iyi idali nthawi yoyenera kuti ana a anthu ake adzipita kwao ndichifukwa chake adapanga moyo wao kukhala ovuta kuti anthu akhale ndi khumbo lobwerera kwao. Inali nthawi yakuti Ahebri apite kukalanda dziko lomwe Mulungu adalonjeza kwa Abrahamu. Vesi 11-14 akunena momwe anthu a ku Igoputo adapangira potsalora ana a Mulungu kuti abwerere kwao.

Kenako muvesi 15-11 Farao adalamulira kuti mwana aliyense wamwamuna wongobadwa kumene wa Ahebri aphedwe. Zinthu zonga zomwezo zidachitika zaka 1500 za kutsogolo kwake pamene Yesu adabadwa, onani Mateyu 2:16.

Timaphunzira phunziro mu makhalidwe a chikhristu, kuchokera munkhani imeneyi ndipo nkhaniyi ikufanana ndi nkhani ya Rahabu yemwe adali hule. Phunziro ndilakuti kunama ndi tchimo mwanjira ina iliyonse kupatula panfundo imodzi yokha yomwe imaonetsa kuti kunama sitchimo. Nfundoyi ndiyakuti timaloledwa kunama, kapenanso kulamulidwa, kunama ngati kunamako kungathandidze kupulumutse munthu otsachimwa kuti asaphedwe. Chifukwa kupha ndi tchimo lalikuru kwambiri.

Eksodo 1:16 Farao akulamulira anamwino a Chiheberi kupha makanda a chimuna. Muvesi 17 anamwinowa akana kunvera Farao. Muvesi 18 ndi 19 anamwinowa adanama kwa Farao. Mu vesi ya 20 ndi 21 tikuona Mulungu akupereka mphoto kwa anamwinowa chifukwa chatsapha anawa.

Tikaonanso mubuku la Yoswa 2:1-4 Mulungu akutipatsa nkhani ina kuti atiphunzitse ife phunziro lofanana ndi lomwe tikuliona munkhani ya anamwinowa. Vesi 4 ikutiudza momwe Rahabu adanamira kuti atetedze miyoyo ya azondi a chihebri omwe anabitsala m'nyumba mwake. Yoswa 6:25 akutiudza kuti Rahabu ndi banja lake adaloledwa kukhala ndi Ahebri ngati mphoto pazomwe adachita kupulumutsa moyoyo ya ozondawo. Buku la Ahebri 11:13 akunena kuti Rahabu adachita mwachikhulupiriro pamaso pa Mulungu. Yakobo 2:25 akunena kuti kunama idali ntchito ya chikhulupiriro yomwe idalungamitsa Rahabu. Mateyu 1:15 akutiudza ife kuti Rahabu ndi limodzi mwa makolo a Yesu. Tikuona kuti Rahabu anadalitsidwa chifukwa adanama pofuna kutetedza azondiwo.

Kumbukirani kuti sitiyenera kunama pokhaokha pamene tikufuna kupulumutsa moyo wa munthu otsalakwa kuti asaphedwe.

Mutu 2:1-10 akunena momwe Mose adapulumukira ku imfa napita kukaleledwa ndi mwana wamkazi wa mfumu Farao. Mulungu adakonza zinthu kotero kuti amatsamalilidwa ndi mayi omubereka ndipo mayi wakewa amalipidwa ndi pochita izi ndi mwana wamkazi wa Farao. Mose adakula ndikuphunzira m'nyumba ya Farao. Adakhala zaka 40 akukhala m'moyo wodala m'nyumba ya mfumu ngati mwana wa ku banja lachifumu.

Mutu 2:11-15 Mose adadzindikira kuti Iye ndi mu Hebri ndipo adakhala okwiya pamene adaona kuti mu Igoputo akumenya mu Hebri kotero adakwiya kopotsa mpaka adapha mu Igoputoyo. Chifukwa chakuphaku zidamupangitsa Mose kukakamidzika kuthawa mu Igoputo. Adathawira ku Midiyani (komwe lero ndi ku Saudi Arabia) ndipo kumeneku adapedza banja nakwatira mwana wa Yetero ndi kukhadzikika kwa zaka 40. Komabe Ahebri adazunzidwabe ku Igoputo.

Mutu 2:16-4:17 tikunva nkhani ya Mose kuti adakhala muchipululu kwa zaka 40.

Mutu 3:1-6 Mose akukumana ndi Mulungu, izi ndizomwe zimatchedwa Mulungu kukhala ngati munthu (theophany)—pamene Mulungu adaonekera kwa Mose mu njira yomwe idapangitsa Mose kudziwa kuti Mulungu ali pakati pake. M'mbuyomo izi zidachitika kwa Abrahamu ndi Yakobo. Kumbukirani kuti Mulungu ndi Mzimu;

ndiotsaoneka ndimaso. (Akolose 1:15) Mulungu nthawi zambiri adali kukumana ndi anthu amene adafuna kuwagwiritsa ntchito pazolinga zake. Mulungu amalora anthu amenewa kuona chinachake choimirira kupedzeka kwake, chifukwa ife anthu, muthupi lathu lochimwa sitingaloledwe kuona nkhope ya Mulungu. Vesi 7:10 mulungu akuyitana Mose kutsogolera anthu ake kutuluka mu Igoputo kupita ku dziko la lonjezo. Onani mutu 3:11 kuti muone kuyankha kotsayenera kwa Mose pa zomwe Mulungu adamuudza. Onani Yesaya 6:8 kuti muone m'mene anthu akhulupirira amayankhira Mulungu akawaitana. Mathero onse a mutu 3 tikuona Mose ndi Mulungu akutsutsana zokhudzana ndi kuti Mose akatulutse anthu a Mulungu mu dziko la Igoputo.

Mutu 4:1-5 tikuonabe kupitirira kwa nsutso wa Mulungu ndi Mose omwe pamapeto pake udakwiyitsa Mulungu. Kotero Mulungu adatsankha Aroni kuti akhale omuyankhulira Mose, ndipo Mose adabwerera ku Igoputo. Adawaudza anthu kuti Mulungu akudziwa kutsauka kwawo ndipo akufuna kuwaombola iwo ku ukapolo. Vesi 31 akunena kuti anthu adali okondwera atanva izi.

Werengani Eksodo 4:24-26 kuona chitsanzo chamomwe tinganvere Mulungu. Zikuonetsa kuti Mose sadanvere Mulungu, ndipo sadachite m'dulidwe kwa mwana wake.

Eksodo 5 nkhondo ikuyamba pakati pa Farao ndi Mose. Mose apempha Farao kuti alole anthu ayende ulendo wa matsiku atatu wakuchipululu kuti akalambire Mulungu wao. Yankho la Farao mu vesi 6-9 kudali kuyenjedza ntchito kwa anthu kuti ikhale yokhwima kwambiri. Vesi 21-23 anthu akuonetsa kuti chikhulupiriro chao mwa Mulungu chachoka monga m'mene amachitira kutsogolo komwe tikupitaku ndipo amadandaula kwa Mose, ndipo Mose adazuzula Mulungu. izi ndi zinthu zomwe sitiyenera kuzichita. Zimaonetsa kuchepa kwa chikhulupiriro.

Eksodo 6:1-8 Mulungu sadaonetsere mkhwiyo wake pa anthuwa. Akupanga onjezo lakuti awaombola iwo ku ukapolo ndikuwapititsa ku dziko la Kanani lomwe adzapereke kwa iwo. Akulonjezanso kuti adzakhala Mulungu wao. Adayankhula izi Mose ndi anthu onse atamugalukira, zomwe zikuonetsa kuti Mulungu ndi wachikondi wokhulupuka komanso osapsa mtima msanga.

Eksodo 6:28-12:30 akunena za mlili yokwana khumi yomwe idali nkhondo zokwana khumi pakati pa Farao ndi Mose. Werengani mutu 8:1-15 momwe zidathera pakati pa Mose ndi Farao. Mulungu kuzera mwa Mose adachita zozizwa kenako amasenga a Farao, kudzera mu mphamvu ya Satana, adachitanso chimodzimodzi. Ili ndi phunziro kwa ife kuti Satana adalinso wamphamvu munthawi ya Mose ndipo alichomwecho lero. Tikuona pamapeto pa mulili uliwonse, kuti Mulungu amaumitsa mtima wa Farao zomwe zimapangitsa Farao kukanitsitsa kulola ana a Israeli kuti amuke. Eksodo 4:21 tikuphunzirapo kuti Mulungu ali ndi mphamvu zonse ndipo ndi Mulungu yemweyo amaumitsa mtima wa Farao kuti akane pempho la Mose.

Mulili otsilidza ukuonetsedwa pamutu wa 12 udali oopsa kwambiri; kudali kupha kwa mwana woyamba wamwamuna mu Igoputo pakati pa zoweta ngakhalenso anthu. Ichi ndichomwe pamapeto pake chidapangitsa Farao kulora Ahebri kuti apite kuchoka ku Igoputo.

Nkhani ya Pasika ndi nkhani ya momwe mwazi wa nkhosa yosachimwa umapakidwa pakhomo la nyumba kuti upulumutse okhala m'nyumbamo kuimfa. Nkhosa ya pa pasika imalodzera kuchipulumutso chathu chomwe. Ndi mwazi wankhosa yotsachimwa ya Mulungu, Yesu Khristu womwe ukupulumutsa akhristu ku imfa yamuyaya ku Gahena. Kumbukirani kuti Baibulo limati pa Hebri 9:22 popanda kukhetsa mwazi palibe chikhululukiro cha machimo.

Eksodo 12:1-20 mulungu akupereka malangizo amomwe Ayuda adzidzakumbukira mwambo wa pasaka mtsogolo mwao.

Eksodo 12:29 akunena kuti pakati pa utsiku ana onse oyamba a mu Igoputo adaphedwa, m'nyumba ina iliyonse yomwe mwazi wankhosa sudapakidwe pakhomo la nyumbayo. Monga momwe Mulungu amaonera mwazi pa khomo la Nyumba ndikutsiya banjalo osaliononga chomwechonso lero kuti Mulungu akuona mwazi wa Yesu ukukuta a Khristu ndikutipulumutsa ife ku imfa yachiwiri yomwe ndi Gahena.

Ahebri tsopano akuchoka ku Igoputo. Eksodo 13:17-22 akunena momwe mulungu mwini adatsogolera anthu ake, mu ntambo njo utsana ndi moto utsiku. Vesi 19 ikunena momwe anthuwa adachitira pokumbukira pempho la Yosefe potenga mafupa ake pamene amachoka mudzikoli. Genesis 50:25.

Eksodo 14:4 akunenanso kawiri kuti mulungu adaumitsanso mtima wa Farao amene anaganidza kuti akutsatira Ahebri. Vesi 10-12 akunenanso za kudandaula kwa Ahebri kwa Mulungu.

Eksodo 14 ndinkhani yakuoloka nyanja yofiira. Farao amaganidza kuti waapedza Ahebri chifukwa cha nyanja yomwe idali kutsogolo kwao ndikuti alephera kuoloka, koma Mulungu adapereka mphamvu kwa Mose pamene adalekanitsa madzi a m'nyanja ndikulola Ahebri kuti aduse. Kenako adapanga madzi kuti abwerere momwe adalili pamene adamedza a Igoputo onse.ndibweredzenso kuti Mulungu amakonza pobitsalira pa anthu ake. Vesi 31 akutiudza momwe Ahebri adakhulupiriranso Mulungu.

Mutu 15:1-12 akunena za momwe anthu adasangalalira ndi kuyimba komanso kuvina potamanda Mulungu. Iyi imadziwika ngati nyimbo ya Mose. Anthu adakonda Mose ndi mulungu kufikira pamene adakumananso ndi vuto lomwe likupedzeka mu vesi 22-24. Tikuona kuti anthunso adalibe chikhulupiriro mwa Mulungu, ndipo nthawi zambiri zinthu sizidali monga iwo amaganidzira ndipo amadandaula motsutsana ndi Mulungu. Vesi 25 akunena momwe Mulungu adaperekera madzi abwino kwa anthuwa kuti amwe.

Mutu 16 akunena momwe Mulungu adaperekera zakudya kwa anthuwa kuchokera kumwamba—monga mana ndi zinziri. Kachiwirinso vesi 1-3 akunena zamomwe anthuwa anadandaulanso motsutsana ndi Mulungu chifukwa adali ndi njala. Anthuwa akuonetsanso kuchepa kwa chikhulupiriro chao mwa Mulungu. Motsayang'anira kudandaula kwao, Mulungu adawapatsa chakudya monga mana ndi zinziri.

Mulungu amapereka tsiku ndi tsiku zotsowekera monga momwe zikufunikira nthawi imeneyo. Anthuwa adaphunzitsidwa kukhulupirira Mulungu ndikusonkhanitsa patsiku chakudya chomwe chingawakwanire kungopatula tsiku la Sabata. Mulungu adali kupereka chakudyachi kufikira pamene anthuwa adakalowa m'dziko la malonjezo.

Mutu 17 anthuwa adatsutsananso ndi Mose komanso Mulungu chifukwa amafuna madzi. Kenako anafika Ku phiri la Sinai, komwe adakhala kwa nthawi yaitali ndipo Mulungu adawaphunzitsa momwe angamupembedzere Iye komanso kukhala m'moyo onvera malamulo ake.

Mutu 19 ukuyamba kunena za za gawo lachiwiri la buku la Eksodo pamene Mulungu akuyamba kuphunzitsa anthu. Kuphunzitsa kumeneku kukupitilira mpaka mubuku la Deuteronomo kufikira anthu kulowa m'dziko la malonjezo. Mulungu akuphunzitsa Ahebri zamomwe angakhalire monga anthu ake—anthu otsiyana ndi dziko lapansi. Ahebri adali achikunja pamene amakhala ku Igoputo, ndipo amafunikira kuwaphunzitsa zokhudzana ndi Mulungu wao.

Monga chipangano Chakale chikutiphunzitsa kuti anthu a Mulungu adali otsiyana ndi dziko lapansi, koteronso Chipangano Chatsopano chikutiphunzitsa kuti akhristu akuyenera kukhala motsiyana ndi dziko lapansi. Chidzindikiro chimodzi choonetsa kuti Ayuda adali otsiyana ndi dziko lapansi chidali chakuti amuna onse a ntundu wao amalandira m'dulidwe, onani Genesis 10-14. Lero akhristu onse amabatidzidwa chomwe ndi chizindikiro kuti ibfe ndi akhristu; ndipo ichi chimatipanga kukhala opatulidwa kudziko lapansi.

Mutu 20-23 Mulungu akupanga pangano ndi anthu pamene akuwapatsa lamulo ndikulonjeza dalitso akamvera lamulo.

1.pali malamulo amitundu itatu omwe adapatsidwa kwa anthu a mu Chipangano Chakale. Awa amaziwika kuti:

A. Malamulo a chipembezo. Awa ndi Malamulo amene amadziwitsa Ayuda zamomwe angapembedzere Mulungu munthawi ya Chipangano Chakale. Malamulowa amawatsogolera anthu m'mene angapembedzere mukachisi ndikupereka msembe. Akhristu sayenera kumvera malamulowa chifukwa sitiri pansi pa Pangano lakale ndipo sitimalambira Mulungu monga ankachitira anthu a mu Chipangano Chakale. Akhristu lero tili pansi pa Pangano latsopano.

B. Malamulo a boma. Ndi Malamulo amene amanena zamomwe boma lingalamulire anthu ake. Sitimatsatira malamulo amenewa chifukwa adapangidwa kuti alamulire a Israeli akale.

C. Malamulo achikhalidwe ndi omwe tiyenera kuwamvera mpakana lero lino. Malamulowa amatiudza momwe tingamvera Mulungu. Malamulo khumi a Mulungu tikuyenera kuwamvera.

2. Mulungu adatipatsa Malamulo khumi amene ali ndi ulamuliro pa ife mpaka lero. Tiyeni tione malamulowa.

<u>Malamulo khumi a Mulungu</u>

1. *Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha.* Lamuloli likunena za yemwe tikuyenera kumupembedza. Izi zikutanthaudza kuti tikuyenera kupembedza Mulungu m'modzi yekha wa Chipangano Chakale.

2. *Usazipangire wekha fano losema kapena chifaniziro cha thambo lakumwamba kapena cha pansi pa dziko, kapena cha madzi a pansi padziko. Usazipembedzere izo; usazitumikire izo.* Lamuloli likunena za momwe tingapembedzere. Sitiyenera kupembedza zinthu zooneka ndi maso kapena mtanda.

3. *Utsatchule dzina la Yehova Mulungu wako pachabe, pakuti Mulungu sadzamuyetsa iye osachimwa amene atchula pachabe dzina lakelo*. Nthawi zonse tigwiritse ntchito dzina la Mulungu mwa ulemu. Musaligwiritse ntchito dzinali pazokambirane zopanda pache. Chitsanzo chakugwiritsa ntchito dzina la Mulungu pachabe ndipamene munthu wapunthwa amvekere "O Mulungu wanga."

4. *Uzikumbukira tsiku la sabata likhale lopatulika.* Ndilapadera kuti ife tipite kutchalitchi ndikupangira limodzi mapephero. Kuchita ntchito zachifundo ndikukhala pamodzi ndi banja lathu.

5. *Uzilemekedza atate ako ndi amako kuti achuluke matsiku amene Mulungu wako akupatse iwe.* Izi zikutanthaudza kuti tikuyenera kulemekedza achikulire onaninso Levitiko 19:32.

6. *Usaphe.* 1 Yohane 3:15 akutiphunzitsa kuti kumuda m'bale wathu ndi kupha.

7. *Usachite chigololo.* Pakuganidza ndi kupenya ndinjira zina zomwe ungapangire chigololo ndi kuphwanya lamuloli onani Mateyu 5:28

8. *Usabe.* Pali zitsanzo zambiri zakuba monga kufuna malisiti andalama zochuluka kupotsa zomwe wagwiritsa ntchito, ulesi pochita ntchito yomwe malipiro ake watenga kale.

9. *Usam'namizire mzako.* Osanama; kunama kulibe nsinkhu, chifukwa bodza lililonse ndiloopsa kwambiri. Bodza limodzi limachotsa chikhulupiriro mwa iwe kwamuyaya.

10. *Usasirire Nyumba ya mzako. Kapena mkazi wa mzako, kapena wantchito wake wamwamuna kapena wantchito wake wamkazing'ombe yake kapena bulu wake, kapena Kanthu kalikonse ka mzako.* Ukuyenera kukhala okhutitsidwa ndi chilichonse chomwe Mulungu wakupatsa.usachite Nsanje pamene munthu wina akulemera kupotsa iwe. Sikulakwa kupempha kwa Mulungu zinthu ngati galimo yatsopano, komabe ukhale okhutitsidwa ngakhale galimoto latsopanolo sudapatsidwe. Usachite Nsanje pamene mnasi wako wagula Kanthu kalikonse katsopano.

B.Mulungu kupitilidza mpaka mutu 24 kupereka Malamulo otsiyanasiyana okhudzana ndi momwe angakhalire (monga Malamulo a sabata komanso okhudzana ndi kapolo).

Mutu 25-31 Mulungu akupereka malangizo mwasatanesatane amamangidwe a likasa lomwe ndi tenti yaikulu momwe mungamakhale Mulungu pamodzi ndi anthu. Mau oti likasa amatanthaudza malo okhala werengani 25:8 imene ikutiudza kuti likasali ndi

malo amene Mulungu azikhala ndi anthu ake. Vesi 9 ikutiphunzitsa kuti akunenetsa zokhudzana ndi malo omwe angamakhale ndipo zambiri m'mabuku akutsogolowa akuika chitsimikidzo pa malangizo a momwe likasi angalipangire. Tikuphunzira kuti Mulungu watiudza momwe tingafikire kwa Iye moyenera. Akupereka momveka bwino zokhuzana ndi mamangidwe komanso makometseredwe a likasa ndi zovala za amsembe. Mulungu akuonetsa kuti akufuna ife tikonzekere moyenera pofuna kumulambira Iye.

Mutu 32 anthu akuonetsa mtima wao weniweni chifukwa pamene Mose amachedwa ndi Mulungu, anthu adapanga mwana wa ng'ombe wagolide ndikumulambira iye; vesi 1-6 onse awiri Mulungu ndi Mose adakwiya kwambiri. Vesi 7-14 akunena kuti Mulungu adaopsedza kuti awononga anthu onse ndukuyambiranso kawiri. Kawirinso tikuona munthu akupikitsana ndi Mulungu. Vesi 14 ikunena kuti Mulungu adakhululuka ndipo adawarekerera Ahebri osawaononganso.

Vesi 19-20 akunena kuti Mose adapsa mtima ndipo tikuona zomwe adachita. Vesi 26-28 tikuona chilango pa anthu chifukwa cha tchimo pamene anthu okwana 3000 adaphedwa.

Mutu 33:18-23 akunena kuti Mose adapedza chisomo pamaso pa Mulungu ndipo kachiwiri Mulungu adamulola Mose kuti amuonenso. Mose adakumananso ndi Mulungu ndipo adapatsidwanso malangizo a momwe Ahebri angakhalire ndi moyo. Dziwani kuti ngakhale Mose adapeza ufulu pamaso pa Mulungu, komabe Mulungu adamulanga patsogolo pake chifukwa chakusamvera posamulola kuti akalowe m'dziko lamalonjezo.

Mutu 35 akulongosola momwe anthu ankaperekera kwaulere golide wao ndi zinthu zina zofunikira kwa Yehova kuti zigwiritsidwe ntchito pomanga likasa. Zinthuzi adatuluka nazo mu Igoputo zomwe Mulungu adalonjeza mu Genesis 15:14.

Mulungu adapereka malangizo a momwe angamangire likasa ndi momwe angapembedzere Mulungu. Malangizo amenewa, akutiphunzitsa kukhala osamala za momwe tingafikire amaso pa Mulungu. Malangizowa akutiphunzitsanso kuti anthu a Mulungu ndiotsiyana ndi anthu enawa ndipo akuyenera kukhala motsiyananso. Izinso zili chimodzimodzi ndi akhristu; tikuyenera kukhala molingana ndikuti ndife a Yesu Khristu.

Anthu samaloledwa kulowa m'malo moyeretsetsa kukumana ndi Mulungu. Wansembe yekha ndiyemwe amaloledwa kulowa m'malo oyeretsetsa pachaka kamodzi, potenga nsembe yamwazi pofunafuna chikhululukiro cha machimo ake ndi a anthu. Iyi siidali nsembe yangwiro kotero idayenera kuti izichitikchitika. Patsogolo pake Yesu adakhala nsembe yangwiro kotero sikuyenera kuperekanso nsembe ina pamwamba pa iyi.

Ife akhristu tili ndi mwayi kuti tikukwanitsa kukumana ndi Mulungu nthawi ina iliyonse, usana ngakhalenso utsiku ndikuyankhula ndi Iye pa ife tokha. Sitisowanso wansembe wamkuru kuti akhale nkhala pakati wa ife ndi Mulungu chifukwa Yesu ndi Wansembe Wankuru.Yesu adalibe tchimo zomwe zikutanthaudza kuti nsembe Yake pantanda ikhale ya ngwiro yovomerezeka ndi Mulungu Atate ngati dipo la machimo. Zikutanthaudzanso kuti sipadzakhalanso msembe ina pamwamba pa Msembeyi.

Exsodo akumaliza pa Mutu 40:34-38 ndi nkhani yabwino yokhudzana ndi kuzaza kwa ulemerero wa Mulungu ku likasa lomwe lili pamalo pamene Yehova amayankhula ndi ana anthu ake onani Levitiko 1:1.

BUKU LA LEVITIKO

Mutu wa Levitiko ndi ganizo lakuti mukhale oyera—1 Petro 1:16 ndi Levitiko 11:44-45.

Levitiko akupitiridza nkhani yomwe yayambika mu Eksodo maka pa Phiri la Sinai. Mulungu akuphunzitsa Ahebri momwe angakhalire m'moyo osangalatsa Mulungu, ndimomwe angakhalire anthu ake. Ahebri azikhala monga anthu opatulika pamaso anthu ena onse. Ife akhristu tikuyenera kukhala otsiyana ndi dziko lapansi (Yohane 15:19). Anthu a mulungu akuyenera kukhala molingalira za Mulungu. Akhristu amalingalira zokakhala muyaya osati mudziko lino lapansi. Kwathu kwenikweni ndi kumwamba komwe tikakhale ndi Mulungu. Mkhristu akapedza mphoto yake kumwamba, pamene omwe Sali akhristu mphoto zawo alandiriratu pansi pompano.

Malamulo adaperekedwa kwa Ahebri kuti aziwe zimene Mulungu akuyembekedzera iwo kuti achite. Akanvera lamulo mwa ngwiro iwo akalowa kumwamba ndi ntchito zawo zabwino ndipo sadzasowanso Mpulumutsi. Koma palibe munthu angasunge Malamulo a Mulungu mwa mngwiro, kotero tikusowekera Yesu Khristu kuti atipulumutse ku machimo athu.

Kuwerenga buku la Levitiko kumakhala kosapatsa chikoka koma muli ziphunzitso kwa ife. Timaphunzira kuti;

1. Mulungu wathu ndi zanja la Mulungu, m'mawu ena izi zikutanthaudza kuti Mulungu ali okangalika m'miyoyo yathu.

2. Mulungu amaonetsetsa momwe ife timamupembedzera Iye, ndipo timapedza malangizo ambiri a m'mene tingapembezere. Malangizo omwe ndiofunikira ku mpingo lero lino.

3. Padali kutsiyana kwa nsembe pakati pa anthu a Mulungu ndi anthu wamba.

A. Anthu amitundu amapereke msembe kuti awone za kusogolo komanso asangalatse milungu.

B. Ahebri amapereka nsembe kufunitsitsa kuti akhale oyera. Idali njira yofunafuna chikhululukiro cha machimo awo. Chipangano Chakale chimalodzera ku nsembe yopambana komanso yosiridza ya Yesu Khristu.

4. Alevi amatumikira ngati ansembe a Chipangano Chakale, ndi wamkuru wa ansembe yekha amene amalowa ku malo opatulikitsitsa kukakumana ndi Mulungu. Pano tili ndi Yesu Khristu amene ali wa nsembe wamkuru (Ahebri 5:5) ndipo sopano ife akhristu titha kukumana ndi Mulungu nthawi zonse (Ahebri 4:14-16).

A. Ife akhristu tili ndi mwayi zomwe zikutanthaudza mwachitsanzo kuti Mulungu ali okonzeka nthawi zonse kukumana nafe m'mapemphero. Izi sichimodzimodzi ndi achikunja chifukwa alibe mwayi okumana Mulungu, onani Yesaya 59:2 ndi Yohane 9:31. Achikunja angakumane ndi Mulungu pamene alapa tchimo ndi kukhulupirira Yesu Khristu.

5. Sitisowekeranso nsembe koma timadziwa pamene tiphunzira za nsembe. Levitiko amatiphunzitsa kufunika kwa mwazi kuti ukachose machimo. Onani Levitiko 17:11. Chipangano Chatsopano chimatiphunzitsa mu Ahebri 9:22 ndi 1 Yohane 1:7 kuti palibe

chikhululukiro cha machimo popanda kukhetsa mwazi. Mkhristu amalandira chikhululukiro cha machimo ake kuchokera mu kukhetsedwa kwa mwazi wa Yesu Khristu.

Ndichifukwa ninji timaphunzira malamulowa? Akhristu ambiri amati sitifunika kuphunzira malamulowa chifukwa sitili munthawi ya chilamulo. Ndizoona kuti sitizaweruzidwa ndi lamulo komabe tikuyenera kunvera Malamulo a chikhalidwe monga Malamulo khumi a Mulungu. Tikuyenera kuphunzira ndi kunvera kwanthunthu Malamulo maka a iwo amene anena za moyo wathu wa lero. Malamulo amene nthawi zonse akhala amagwira ntchito monga omwe akupedzeka ku Deutronomo 25:4 ndi 25:13-16, Exsodo23:5 ndi 1-9 ndi Levitiko 25:14.

Maphunziro ofunika kwambiri a Levitiko

1. Mulungu ndi oyera pamene anthu ndi ochimwa. Uchimo wathu ndi vuto lalikuru lomwe lafikira anthu onse. Uthenga wa Levitiko ndiwakuti muli chikhululukiro ndi kusukidwa kwa machimo zomwe zimatithandidza ife kukhala mu ubale ndi Mulungu.

2. Malamulo. Levitiko ndi buku lozaza ndi malamulo mu Baibulo lonse. Muli malamulo otsiyanasiyana amene aikidwa ndi Mulungu kuti atitsogolere kwa Khristu kotero kuti tikathe kulungamitsidwa ndi chikhulupiriro. Agalatiya 3:24 malamulo a Mulungu amaonetsa kunyasa koperewera kwa munthu ndi kutisusa za machimo athu. Kunvera malamulo a Mulungu ndi njira yabwino kuti ife tikhale ndi moyo.

A. Tikuona Malamulo a Aisraeli okhuzana ndi zoyenera kudya komanso zotsayenera kudya. Kenako m'Machitidwe 10:10-16 tikuona kuti akhristu tsopano akutha kudya china chilichonse chomwe akufuna.

3.Zopereka zokwana zisanu. Levitiko 1-7 akunena za zopereka kwa Mulungu. Pali zopereka zokwana zisanu. Zimenezi ndi;

A. Za nsembe yopseredza (mutu 1:3-7) anthu adazikhuthura kwa Mulungu kudzera m'moto woyeretsa.

B. zopereka za ufa ndi za zipatso (mutu 2:1-16) kuthokoza Mulungu chifukwa cha moyo wao ndikupereka moyo wao kumutumikira Iye.

C. Mtendere (3:1-17) kutenga gawo mu dalitso la chiyanjano ndi Mulungu.

D. Tchimo (4:1-5:13) kukhululukidwa chifukwa iwo ndi ochimwa.

E. Kulakwitsa (5:14-6:7) pokhululukidwa machimo omwe adachita.

4. Mutu 6:8-7:36 ndi mitu yokhuzana ndi unsembe ndipo ndi mitu ya ansembe a chipangano cha kale.

A. Ntchito ya ansembe mu Chipangano Chakale idali yofunikira kwambiri chifukwa ansembe adali amkhala pakati pa Mulungu ndi anthu ake. Ndichifukwa pali malangizowa mwasatanesatane okhudzana ndi ansembe m'mbuku la Levitiko. Lero Khristu akugwira ntchito ngati mkhala pakati ndipo akutilola ife mosavuta kuti tikumane ndi Mulungu.

B. buku la Ahebri lili ndi phunziro labwino lomwe likufananiza ansembe a Chipangano Chakale, omwe adali ochimwa ndi wansembe wa Chipangano Chatsopano, amene ali wansembe wankuru ndi wangwiro-Yesu Khristu.

C. Lev.7:31-36 mulungu akupereka njira momwe a nsembe angamadyere pa moyo wao wa tsiku ndi tsiku. Tisatilenso chitsanzo ichi ndi kuonetsetsa kuti abusa athu tikuwadyetsa tsiku ndi tsiku.

D. Tikuona pa mutu 8:1-4 kuti mulungu adalamula za kusankhidwa kwa Aroni ndi ana ake kukhala ansembe. M'mau ena, Mulungu adawaitana iwo monga amatiinanira ife ku ntchito ya ubusa kapena ntchito ya ukuru wampingo. Onetsetsani kuti mwaitanidwa ndi Mulungu osati kuziitana inu nokha.

E. Mutu 10:1-2 ana a Aroni adaphedwa ndi Mulungu chifukwa sadanvere Mulungu m'mapembezedwe awo. Tikuyenera kudza kwa Mulungu mwaulemu ndi mtima wolapa. Ndiganizo labwino kuyamba mwambo wachipembezo ndi pemphero la kulapa.

5.Za Tsiku Lotetezera mutu 16.

A. Ili lidali tsiku lofunikira kwambiri kwa a Israyeli chifukwa ili lidali tsiku lomwe chikhululukiro cha machimo chimafika pachimake penipeni. Lidali tsiku lokhalo pachaka kuti wansembe wankuru amalowa muchipinda choyeretsetsa cha mu hema okumaniranako. Ili lidali tsiku lopatulika,mwachitsanzo, lidali tsiku lokhalo muchaka lomwe kusala kudya kudali kofunikira ndithu.

i. Levitiko 16 akutiuza zakutengedwa kwa mbuzi ziwiri. Mbuzi imodzi imaphedwa ndipo inayi mwachithunzithunzi chabe imatenga ndi machimo a anthu onse ndipo imaingitsidwa kupita kunja kwa chigono, itatenga machimo onse a anthu. Vesi 21-22 akutiuza za kuchotsedwa kwa machimo mwa njira yotere.

B. Tsiku lotetedzera lidachosedwa m'malo mwake mudalowa nsembe yotetedzera ya Ambuye wathu Yesu Khristu kuti machimo athu akakhululukidwe.

6.Nthawi yopatulika nyengo zoikika ndi Yehova mutu 23-25.

A. Mulungu adaikiratu matsiku opatulika pamene anthu adayenera kuti alingalire zokhuzana ndi Iye. Matsiku a tchuti amene tili nawo matsiku ano gwero lake ndilimeneri. Akhristu ambiri amasangalala ndi tchuti cha Khrismasi komanso cha pasaka (Easter). Ku United states of America (ku Amereka) akhristu amasangala ndi Kuthokoza chifukwa cha tsiku lomwe lidapatulidwa mwapadera kuti athokoze Mulungu.

Muli phunziro looneka m'moyo wathu kuchokera m'buku la Levitiko 20:1-5. Tikuwerenga kuti Mulungu amadana ndi nsembe zopereka ana. Imfa ndi chilango. Dziwani vesi 4-5 ikuphunzitsa zilango zochuluka kwa munthu amene achitira umboni izi ndi kusayetsetsa kuti athese mchitidwewu. Ndikudabwitsidwa ndi momwe Mulungu amanvera ponena za kupereka ana ngati nsembe, mchitidwe omwe tili nawo kuno ku Uganda. Kodi ife akhristu timalorera tchimo loopsa lizichitika popanda kuchitapo Kanthu kuti lithe? Nanga machimo enawo timachita nawo bwanji?

BUKU LA NUMERI

Bukuli lidapatsidwa dzina kuchokera "kuchipululu" komwe ndi malo omwe nkhani ili m'bukuli idachitikira. Septijuenti lomwe ndi buku loyamba mu Chipangano cha Kale kutanthaudzilidwa kuchokera kuchi Hebri kupita kuchiGriki, adatsintha dzinali kuti likhale Numeri chifukwa chiwerengero cha anthu chidachitika.

Iyi ndi nkhani ya anthu omwe adayenda muchipululu kwa zaka 40 chifukwa cha kusanvera kwawo kuphatikizapo Mosendi anthu onse. Numeri amatiphunzitsa kuti Mulungu azalanga tchimo ndipo Yoswa ndi Kalebu a mbadwo umenewo adaloredwa kukalowa mdziko la malonjezano.

Ahebri adayenda miyezi itatu kuchokera ku Igoputo kupita kuphiri la Sinai. Ndipo adakhala kwa chaka chimodzi pa phiripa kenako zidawatengera zaka 40 kuti akafike ku

Moabu komanso kudziko lamalonjezano. Kuchokera ku Igoputo kukafika ku Moabu ndi ulendo omwe ungayende sabata zochepa zedi.

Zigawo zinayi za bukuli.

I.Choyamba tikuona za pa Phiri la Sinai pamene anthu amakonzeka kuchoka ndi kupitilira ulendo malo okhawo amene adapumako kuchokera pa Eksodo 18. Numeri mutu 1:1mpaka mutu 10:10.

1. Kuwerengedwa kwa anthu. 1:1-54.

2. Pa mutu 2:1-4:49 Mulungu akukonza zinthu pakupereka kwa anthu madera omwe angakakhale molingana ndi ntundu wawo, kenako mtundu uli wonse uzalandira malo ake mdera lao. Adalamula a Levi kukhala a nsembe a ntundu uli onse. Mulungu adakonzekeretsa anthu kupita ku dziko lamalonjezano. Komanso adapitiridza kusunga Malamulo onse a chipembezo.

Numeri 3:1-10 akubweredza nkhani ya momwe ana a Aroni adafera chifukwa cha kusanvera kwao pakupembeza Mulungu ndi momwe Mulungu akuchulukitsira nambala ya ansembe pakulamulanso kuti Alevi azikhala ansembe.

3. Kalembera 5:1-8:26

A. Mulungu akuphunzitsa pa mutu 8:25 ndi 26 kuti Alevi a zaka zopitirira 50 akuyenera kupitirira kuthandidza mu ntchito zonse zopembedzera Mulungu koma asadziyetse kuti iwonso ndi atsogoleri. Ife atsogoleri a mipingo tikuyenera kuphunzitsa achichepere amene angazalowe m'malo mwathu mtsogolomo. Mbusa aliyense ali ndi nthawi yopuma pa ubusa mosakakamizidwa

4. Zochitika zotsiriza pa Phiri la Sinai 9:1-10:10

II. Gawo lachiwiri la buku la Numeri ndi kupitirira kwa ulendo kuchokera paphiri la Sinai kupita ku Edomu (Mutu 10:11-20:21). Ahebri adakwanitsa kupanga ulendo omwe ukadakhala wa masabata atatu kukhala wa zaka 40 chifukwa cha khalidwe lao loyipa pamaso pa Mulungu.

1. Choyamba tikuona za ulendo opita ku Kadeshi 10:11-12:16.

A. Mutu 11 ukunena kuti anthu adapitiridza kudandaula pamaso pa Mulungu ndi Mose. Mose adafunsa thandizo kuchokera kwa Mulungu. Ndipo Mulungu adapereka thandizoli kwa Mose (Mutu 11:16-17). Mose adasankha akuru okwana 70 kuti amuthandidzire. Kenako mu Chipangano Chatsopano, Mulungu adasankha akuru a mpingo ndi madikoni kuti athandidzire pa ntchito ya mpingo.

B. Mutu 12 ukunena za mlandu omwe amasusana ndi Mose amene adali nsogoleri wosankhidwa ndi Mulungu. Tiyeni tione za kuukira kumeneku.

i. Vesi 1-2 akunena za kuukiridwa kwa Mose amenenso adali ntsogoleri osankhidwa ndi Mulungu

ii. Vesi 3 ikunena kuti Mose adali munthu wofasa komanso adalibe matama ngakhale adali ntsogoleri woposa pamaso pa Mulungu.

iii. Vesi 4-8 ikunena kuti Mulungu mwini wake adamutetedza Mose ndi kuzuzula Aroni ndi Miriyamu chifukwa cha kuukirako.

iv. Vesi 9-10 Mulungu ali okwiya ndipo akulanga Miriyamu.

v. Vesi 12-13 Mose akupempherera miriyamu kuti Mulungu amukomere mtima ngakhale kuti Miriyamuyo adamuukire iye.

vi. Vesi 14-15 Mulungu akumuchitira chifundo Miriyamu pakupanga chilango chake kukhala cha kanthawi kochepa.

2. Nkhani yosatira ikuchitika pa Kadeshi yomwe ikunena za anthu omwe sadakhulupirire ndi kunvera Mulungu ndipo pamapeto pake adalandira chilango. Numeri 13:1-2 Mulungu akutumiza azondi kuti akazonde dziko lomwe pa vesi 2 akunena kuti Mulungu walonjeza kupereka kwa anthu ake. Werengani 3-16 Mulungu adatumiza oyimirira m'modzi m'mitundu yonse ya ana a Israyeri amene amayenera kutenga dzikolo kuti likhale lao. Vesi 25-33 azondawa akupereka za zotsatira zaulendo wao. Kalebu ndi Yoswa adapereka umboni wakuti potsakhalitsa akagonjetsa dzikoli koma azondi enawo adakaika kuti Mulungu angakwanitse kusunga pangano lake lowapatsa anthu dzikoli. Iwo sadakhulupirire mau a Mulungu kuti azatenga dzikoli kuti likhale lao. Iwo adapereka umboni wakuti anthu okhala m'dzikoli ndi amphamvu kwambiri ndipo sangakwanitse kuwagonjetsa zomwe zimaonetsera kusowa kwa chikhulupiriro. Mutu 14 ukunena kuti kuukira kwa anthuku kudakwiyitsa Mulungu kwambiri. Onani vesi 11-12. Tikuona kuti Mulungu akuopseza kuononga ntundu wonse wa anthu. Vesi 20-37 Mulungu akuuza akulu onse kuti chilango chawo chikhala choti palibe amene akafike kudziko la malonjezano. Adzakhala akuyenda muchipululu kwa zaka 40 mpaka akulu onse atamwalira. Vesi 37-38 Mulungu nthawi yomweyo akupha azondi okwana 10 amene sadakhulupirire Mulungu.

3. Kuukira kwa Mose kuonetsedwa. Mutu 20:2-5 tikunva m'mene anthu adakwiyitsira Mose pamene amadandaula Mulungu. Vesi 8-13 Mulungu adamupatsa Mose malangizo apaderadera kuti akayankhule ndi mwala ku Meriba ndipo mwalawo ukatulutsa madzi, koma m'malo mwake Mose adatenga ndodo namenya mwalawo pachifukwachi Mose adalangidwa, pamene adauzidwa kuti sakalowa ku dziko la malonjezo. Mulungu amalanga tchimo lililonse.

III. Chigawo chachitatu chachikuru cha Numeri chikuyambira pa mutu 20:22 mpaka 36:13 ndipo chikunena za kuzungulira kwa ana a Israyeri kwa zaka zokwanira 40 pamene anthu achikurire adali kufa nkati mwa ulendo opanda cholingawo.

1. Chisatira tikuona imfa ya Aroni. Mutu 20:22-29 akunena za imfa ya Aroni.
2. Anthu adayambanso kudandaula pamaso pa Mulungu kotero tikunva nkhani ya njoka ya mkuwa (mutu 21:4-9). Mulungu adatumiza njoka za ululu kuti zilange ana a Israyeli chifukwa cha kuukira kwawo ndipo a Israyeli ambiri adamwalira. Kenako anthu adalapa ndipo Mulungu adapereka njira yowapulumutsira. Mose adaika njoka ya mkuwa pa mtengo ndipo anthu adalangizidwa kuti ayang'ane panjoka yankuwayi kuti akhale ndi moyo. Mu buku la Yohane 3:14-15 Yesu adyerekaza kuti izi zikutanthaudza kuyang'ana kwa Yesu Khristu.
3. Mutu 22-24 tikunva za nkhani yotsangalatsa kwambiri.

A. Mutu 22 mfumu Balaki ya ku Moabu idali ndi mantha ndi Ahebri kotero adafunsa Balamu kuti atemberere Ahebri. Mulungu adamudza Balamu kuti asatemberere Ahebri. Balaki adapitiridza kunyengerera Balamu kuti atemberere ana a Israyeli kotero Mulungu adalola Balamu kuti apite kukakumana ndi Balaki. Koma zikuoneka kuti Mulungu sadafune Balamu kukaonana ndi Balaki. Umboni wa izi tikuona munkhaniyi okhuzana ndi bulu amene adaima panjira otsapitirira ndi ulendo. Mulungu adamuudza Balamu kuti apite koma akangoyankhula zomwe Mulunguyo akamuyankhule.

B. Mutu 23 Mulungu adamuudza Balamu kuti adalitse ana a Israyeli m'malo mowatemberera. Balaki adayetsetsa kuti anthuwa atembereredwe koma Balamu adati sangathe kutemberera Ahebri chifukwa Mulungu akumukakamidza kuti adalitse anthuwa.

C. Balamu pa mutu 24 akunena m'maso mphenya momwe Mulungu wakhala akudalitsira ana a Israyeli. Mu vesi 9 Balamu akubweredza lonjezo la dalitso lomwe Mulungu adapangana ndi Abrahamu.

i. Mulungu muvesi 15-25 adamupanga Balamu kuti anenere kwa Balaki. Adayankhula za kubwera kwa mfumu Davide amene azaononge adani ake onse Amoabu ndi a Edomu. Ulosiwu umanena za Davide amene adzapulumutse anthu ake ndi kuzaononga adani ake a dziko lapansi koma nkhani yonseyi imalodzera za kubwera kwa Yesu Khristu pakupulumutsa anthu ake ku ukapolo wa tchimo.

4. Numeri 27:12-23 Mulungu akusankha Yoswa kuti atenge mpando wa usogoleri womwe Mose adali nawo.

5. Mutu 28-30 tikuona za malangizo ochuluka okhuzana ndi chipembezo.

6. Mutu 36 tikunva kuti anthuwa pamapeto pake akufika ku malo a thyathyathya a Moabu omwe ndi olowera ku dziko lomwe Mulungu adalilonjeza kwa ana a Israyeli.

Buku la Deutronomo

Deutronomo amatanthaudza kuti kuwerenga kachiwiri ka chilamulo komanso litha kutanthaudza malangizo osiridza a Mose.

I.Mutu 1-3 ndi chiyambi. Zaka 40 zadutsa tsopano chitulukireni mu Igoputo ndipo Ahebri tsopano ali mu chigwa cha mtsinje wa Yordani kukonzekera kuti awoloke kupita sidya lina. Mwachidziwikire ulendowu ndi wa matsiku 11 kuchokera kuphiri la Sinai kupita ku Kanani. Koma chifukwa cha kusanvera kwa anthu zinawatengera zaka 40 kuti ayende ulendowu. Mose olimbikitsa, adalimbikitsa anthuwa ndizoyankhula zake, kukonzekera komalidza anthu asadalowe mudziko la malonjezano. Adabweredza Mbiri yao kuchokera pamene adachoka paphiri la Horebu (dzina lina la Phiri la Sinai). Mose adawakumbutsa anthu chilango chomwe chidawafikira chifukwa cha uchimo pakusanvera kwawo. Mutu 1:3 Mose akukumbutsa anthu kuti ulamuliro wake ndiochokera kwa Mulungu ndikuwakumbutsanso kuti mawu amenewa ndi mau a Mulungu.

II. Mose akubweredzanso Malamulo amene anthu adapatsidwa.

1. Mose akukumbutsa anthu pa mutu 4 kuti anvere lamulo ndikusangalala ndi madalitso chifukwa cha kunvera kwao komanso kulangidwa chifukwa cha kusanvera.

2. Mutu 5 malamulo khumi akuonedwanso kawiri. Malamulowa ndi tsinde la lamulo laku United States.

3. Mutu 6 uli ndi phunziro lofunika kwambiri maka pa vesi 4-10 omwe akutilangiza ife kukonda Mulungu ndi mtima wathu wonse ndi moyo wathu wonse ndi mphamvu zathu zonse ndi nzeru zathu zonse. Yesu pa Marko 12 adabweredzanso lamuloli ponena kuti ndilamulo lopotsa zedi. Yohane 14:5 akuti timaonetsa kuti tikukonda Mulungu pamene tikunvera Iye. Tikuyenera kunvera Mulungu kuti tionetse chikondi chathu kwa Iye.

4. Mutu 7:6-8 akunena za tsinde la pangano la ubale wathu ndi Mulungu. Ichi ndi chisankho chopambana cha Mulungu onani Aroma 8:29-30.

5. Tikuona pa mutu 14:21 kumatsulira malemba motsayenera komanso kumanga ziphunzitso motsayenera. Ayuda amagwiritsa ntchito mauwa pophunzitsa kunena kuti Mulungu akuti simungadye nyama ndi zinthu zina zochita kukonza nthawi pankhomaliro imodzi.

6. werengani mutu 18:15-22 pamene pali phunziro lofunikira lokhudzana ndi aneneri. Tikuwerenga kuti Mose adali mneneri weniweni ndipo vesi 15 ikupereka lonjezo kuti Mulungu azautsa mneneri wina zomwe zidachitika ndipo mneneri ameneyi

ndi Yesu. Mu vesi 20, Mulungu akuti aneneri onama azafa ndithu. Vesi 22 akunena kuti tngazindikire mneneri oona pamene zolotsera zake zikukwaniritsidwa. Kodi mneneri woyamba amene akutchulidwa m'Baibulo ndi yani? Onani Genesis 20:7.

III. Mutu 27-30 tikupedzamo ndemanga za Mose zokhudzana ndi kunvera Mulungu.

1. Mutu 27:15-26 pali mndandanda wa matemberero obwera chifukwa cha kusanvera Mulungu.

2. Mutu 28:1-14 pali malonjezo a madalitso chifukwa chakunvera Mulungu onani vesi 1-6 mitu yonse yosatira ikunena zokhuzana ndi matemberero, werengani vesi 15-19 akulonjeza matemberero ndi zilango chifukwa cha kusanvera kwao. Onani Yesaya 57 panfundo yomweyi. Kwambiri timaona zolemba zokhuzana ndi matemberero kusiyana ndi madalitso; zikuoneka kuti Mulungu amafuna kutsimikidza kuti tachenjezedwa mokwanira.

3. Mutu 29 ndi kukonzedwanso kwa pangano lomwe lidachitika paphiri la Sinai mbuku la Eksodo mutu 20-23 pamene Mulungu adawapatsa iwo lamulo ndikulonjeza dalitso akanvera lamulolo.

A. Mutu 29 vesi 29 ndi Yesaya 55:8-9 ndi mavesi ofunikira kwambiri omwe amatithandidza kunvetsetsa kuti ife sitimanvetsetsa chili chonse chokhuzana ndi Mulungu kotero sitingayankhule chilichonse chokhudzana ndi Iye.

4. Mutu 30 Mulungu akukumbutsa anthu kuti ali ndi mwayi osankha moyo kapena imfa. Vesi 16 ikulonjedza moyo kusatira pakunvera ndipo vesi 17-19 ikunena za imfa chifukwa cha kusanvera.

IV. Mutu 31-34 utsogoleri ukulowa mmanja mwa Yoswa.

1. Mutu 34 ukulongosola za imfa ya Mose akadali ndi zaka 120 pamene adali wanthanzi ndithu. Mulungu adamutenga Mose nakwera pamwamba pa Phiri la Pisga ndikumulola kuti aone dziko la malonjezo, koma Mose sadaloledwe kulowa m'dzikoli.

Buku La Yoswa

Bukuli likuyamba chigawo chatsopano cha Baibulo. Gawoli limatengedwa kuti ndi gawo lambiri chifukwa limanena za Mbiri ya ana a Israyeli kuchokera pamene amalowa m'dziko lamalonjezano kufikira nthawi imene Chipangano Chakale chidatha. Chigawochi chimayamba ndi buku la Yoswa ndipo chimatha ndi buku la Estere.

Ndi mabuku onena za chipambano, kugonjetsa komanso buku loonetsa za kulephera kwa anthu.

Bukuli lili ndi zigawo zitatu.

I. Mutu 1-12 tikunva momwe anthu adagonjetsera dzikoli.

1. Mutu 1 mulungu akutuma Yoswa. Vesi 1-9 pali ziphunzitso zofunikira kwambiri kwa ife. (A) Vesi 5-7 ndi 9 tikuyenera kukhala ochilimika pamene tikutumikira Mulungu. Akunena kuti nthawi zonse Mulungu azakhala nafe. (B). Vesi 7-8 tikukumbutsidwa kuti tinvere Mulungu nthawi zonse.

2. Mutu 2 ndi 5:13-6:27 akuyerekedza nkhani ya kugwa kwa Yeriko. Mutu 5:13-15 ikuonedwa ngati kuwonekera kwa Yesu mu umunthu wake asanadze pano padziko lapansi.

A. nkhani ya Rahabu pamene anasunga azondi awiri ndipo adatsiyidwa wamoyo pamene nzinda wa Yeriko umagwa zomwe zikukambidwa pa mutu wa 2.

B. Azondiwa adatsiyana ndi azondi am'mbuyomu aja chifukwa awa adabwerera ndi mau a bwino onani vesi 4.

C. tikunvapo za nkhani yodziwika bwino yakugwa kwa mzinda wa Yeriko. Mulungu adalamulira kuti asilikali azungulire nzindawu kamodzi pa tsiku kwa matsiku asanu ndi limodzi. Tsiku la chisanu ndi chiwiri anthuwa adazungulira mzindawu kasanu ndi kawiri ndipo adakuwa ndipo malinga a Yeriko adagwa. Chuma chonse chimachokera kwa Mulungu ndipo china chilichonse cholengedwa, nyama ngakhale anthu adaphedwa kungopatulapo banja la Rahabu. Chipambano chimenechi cha ku Yeriko ndi nkhani ya kupambana kwakukuru kwa anthu a Mulungu.

3. Mutu 3:1-17 tikunva momwe anthuwa adawolokera Yordani pouma monga momwe adaolokera Nyanja yofiira nthawi zoyamba zija ndipo Mulungu adakwaniritsa lonjezo lomwe adapangana ndi Abrahamu potenga anthu kulowa nawo m'dziko la malonjezano.

4. Mutu 4:1-9 akunena za momwe anthu adamangira chikumbutso kwa Mulungu ndi miyala.

5. Mutu 7-8 tikunva kugonjetsedwa kwa mzinda wina dzina lake Ai. Nkhani ya kusanvera ndi kusokera kwa zinthu ikusogozana ndi kunvera ndi kupambana.

A. Choyamba tikuona nkhani ya kutsanvera kwa Kaini amene adasunga chuma cha ku Yeriko ndipo izi zidapangitsa ankhondo a Yoswa kuluza nkhondo ndi anthu a ku Ai. Akani ndi banja lake lonse lidaphedwa ndipo kenako Ai adagonjetsedwa ndi asilikali a Yoswa.

6. Mutu 9 ukunena zakuputsisidwa kwa ana a Israyeri chifukwa amachita zinthu pa iwo okha osafunsira Mulungu pamene adali kuchita ndi a Gidioni. Izi zimatanthaudza kuti a Israyeli amayenera kukhala ndi Agidioni osawaononganso.

A. phunziro kwa ife ndilakuti kawirikawiri tizifunsira zonse kwa Mulungu kutsiyana ndi kudalira pa ziganizo zathu, onani vesi 14 yomwe ikuti sadafune langizo la Mulungu.

B. Phunziro lina la utsogoleri wabwino. Yoswa adali ndi zofooka zake.

7. Mutu 10-12 tikunva za momwe asilikali a Mulungu adagonjetsera ndi kuwononga maufumu otsiyanatsiyana.

II. Gawo la chiwiri la buku la Yoswa mutu 13-24 akunena za kagawidwe ka dzikoli.

1. Mtundu uliwonse wa ana a Israyeli udalandila cholowa kupatula ana a Levi. Ndichifukwa ninji a Levi sadalandire cholowa?

2. Yoswa 23 akunena za mau a kusazika kwake kwa atsogoleri.

A. Yoswa akunena chifukwa chomwe chidamupangitsa kukhala chida champhamvu pamaso pa Mulungu, komanso akunena za zomwe atsogoleriwa azikwaniritsa. Werengani 3 ndi 5 Yoswa akulemekeza Mulungu chifukwa cha chipambano chomwe adawapatsa. Anthu enieni a Mulungu amathokoza pamene Mulungu wapereka chipambano m'mzanja lawo. Tikumbukire kuti ife anthu sitingapambane nkhondo patokha popanda Mulungu. Timapambana pamene Mulungu watimenyera nkhondo.

B. Adawakumbutsanso atsogoleriwa kukhala okhulupirika pa maso pa Mulungu maka pankhani ya kukwatira akazi a chilendo a kukanani. Adawachenjeza kuti ngati sanvera, Mulungu azaonetsa nkwiyo wake potsutsana nawo. Uwu ndi uthenga ofanana omwe Mose adapereka kwa anthuwa.

3. Yoswa mutu 24:1-13 akukumbutsa anthu za kukhulupirika kwa Mulungu kuti popita nthawi Iye adapereka kwa anthu dziko la malonjezo lomwe adalonjezana ndi makolo awo Genesis 12:7.

4. Vesi 14-18 Yoswa akunena mau ake osiliza kwa anthu ndikuwauza kuti akhale okhulupiririka ndi kutumikira Mulungu yekha. Vesi 15 ndi vesi yodziwika bwino m'Baibulo pamene Yoswa adatsimikidza kuti iye ndi a pabanja pake adzatumikira Mulungu wakumwamba. Anthu onse adalonjedza kuchita chimodzimodzi. Tilongosola m'buku la oweruza momwe anthuwa adasungira lonjezoli.

5. Yoswa adamwalira ali ndi zaka 110 ndipo adaikidwa mmanda a kudziko lamalonjezano.

Buku la Oweruza

I.Chiyambi. olemba ndi nthawi yomwe bukuli lidalembedwa sizikudziwika koma nthawiyi idakhalapo kwazaka 400 ndipo imadziwika kuti nthawi ya mdima ya a Israyeli (monga ku Uganda nthawiyi idalipo mu ulamuliro wa Idi Amin). Ndi nthawi yomwe imalongotsoledwa bwino ndi vesi losiliza la muchaputala chosilizanso cha bukuli (21:25). Ganizo lakuti anthu adayenda munjira zao kutsiya kusata njira za Mulungu likubwerezedwa bweredzedwa mu machaputala oyambirira mubukuli. Yesu adayankhulapo zokhudzana ndi ganizoli: Yohane 14:15 "Ngati mundikonda ine muzasunga Malamulo anga." Ndikuganiza kuti anthu samakonda Mulungu kwenikweni. Kumbukirani lonjezo lao mbuyomo lakuti azanvera Mulungu-adangolonjeza kuti azanvera Mulungu koma sadachite zimenezi.

Oweruza omwe akunenedwa m'bukuli si Oweruza omwe tikuwadziwawa koma ndi asogoleri a nkhondo-akazembe ankhondo. Kachitidwe ka Oweuzawa kadali kakuti anthu amagwa m'machimo ndipo zotsatila zake Mulungu amawaika m'manja mwa adani ndipo pamene aphinjidwa ndi adaniwa amatembenukira kwa Mulungu ndipo Mulungu amawatumidzira Oweruza amene amawathandidza. Adali Oweruza okwana 12.

II. Mutu 1-16 ukunena za oweruza osiyana siyana okwana 12.

1. Vuto loyamba likulongotsoledwa mu mitu yoyamba 1:1-2:5 pambuyo pa imfa ya Yoswa. Anthuwa adalephera kugonjetsa adani awo, kotero sadakwanitse kuchotsa anthu onse okhala mu dziko lija monga Mulungu adawaudzira mu Deutronomo 20:16-18. Ndikusanvera pamaso pa Mulungu pamene tilephera kuchita zomwe watilamula. Tikuyenera kunvera zolamulira zonse za Mulungu osanyalanyaza ayi. Vuto mu buku la Oweruza ndilakuti adawatsiya ndi moyo anthu omwe adawapedza m'dziko la malonjezo omwe amawapangisa a Israyeli kuchita zinthu zoyipa. Chikuyambitsa mavuto ambiri mu mpingo wa kwa azungu ndi kusanvera Mulungu komanso kunyalanyaza Malamulo amene Mulungu adatipatsa. Chitsanzo ndichakuti Mulungu adatilamula ife kuti tisamakwatire anthu amene asali akhristu. Koma akhristu kawirikawiri amakankhira izi kunkhongo pokwatira anthu omwe si akhristu komwe kuli kusanvera Mulungu. Nthawi zambiri mabanjawa amapangitsa akhristu kutsiya kutumikira Mulungu; kawirikawiri

nkhristu amatsiya kupita kutchatchi. Ndipo ana obadwa mbanjali amaleredwa munjira yachikunja osati ya chikhristu.

2. Werengani 2:1-5 kusanvera kwa Israyeli ndi ulosi wa masautso a ntsogolo chifukwa cha kusanvera. Iyi ndi nkhani yomwe yamanga nthenje m'Baibulo lonseli.

A. Mutu 1 vesi 1 ndi Mulungu kuoneka ngati munthu (theophany). Onani Exodo3:2-6.

3. Mutu 2:6-16:31 ndi nkhani za kulephera kwa Israyeli. M'badwo wonse wa Yoswa wamwalira tsopano, ndipo m'badwo wotsatira ukukana Mulungu.

A. Onani 2:10. Tikuona kuti m'badwo watsopano sumadziwa Mulungu. Ili lidali komanso ndi vuto mu mpingo lero. Onani Deutronomo 4:10 kuti tione mavesi ambiri omwe Mulungu akutiuza kuti tiziphunzitsa ana athu zokhuzana ndi Mulungu.

Ndondomeko iyi ikubwerezedwabwerezedwa mu buku la Oweruza:

1. Anthu amachimwa pamene Israyeli wachita zoipa pamaso pa Mulungu.
2. Nkhondo ngati chilango. Mulungu amawapereka iwo m'manja mwa adani awo adziko lina kwa zaka zambiri ndipo ankazuzika kwambiri.
3. Kenako anthuwo amalapa ndikulira pamaso pa Mulungu kuti awapulumutse iwo ku mavuto.
4. Kumasulidwa kumabwera pamene Mulungu amazutsa wopulumutsa (Oweruza) amene amawapulumutsa. Ndipo dzikoli limakhala ndi ntendere kufikira pamene anthu ayambiranso kuchita uchimo.
5. Kuzungulira kwa uchimoku kumasogozana ndi kulapa kenako kulanditsidwa kenako kuchimwanso kawiri ndipo izi zakhala zikuchitika motero kwa zaka zokwana 400.

Oweruza ena adali abwino pamene oweruza ena adali oyipa.

Debora adali Oweruza wabwino ndipo amayamika Mulungu kwanthunthu pakupambana kwake (5:1-9 ndi 31).

Gideoni adali oweruza wabwino amene nthawi zambiri amakhala ndi vuto lauchimo. Pamene tikuphunzira za Gideoni tiona nfundo yakuti "Mulungu amathandidza amene ayamba kuzithandidza okha" kuti ndiyolakwika kwambiri. Tiona kuti Mulungu amatenga anthu ofoka ndikuwapatsa mphamvu zochitira zinthu zamphamvu.

A.Gideoni adaitanidwa ndi Mulungu kuti atsogolere anthu a Mulungu amene amasautsidwa ndi Amidiyani. Mutu 6:1-27 Mulungu muvesi 12 adamutchula Gideoni kuti ndi munthu wanyonga koposa. Koma Gideoni adani iye siwamphamvu kwenikweni chifukwa akuchokera ku mtundu wofoketsetsa mu fuko lao lonse ndipo kuti iye ndiwang'ono kopotsa m'banja lakwawo malingana ndi vesi 15. Mu vesi 16 Mulungu akumuuza Gideoni kuti azakhala wamphamvu chifukwa Iye (Mulungu) azamupatsa mphamvu kotero Mulungu pamapeto ndi amene azalandire ulemerero osati Gidiyoni.

B.Mulungu akufuna kuti Gideoni atsogolere asilikali ake kukalimbana ndi asilikali aku Midiyani. Gideoni akuoneka kuti chikhulupiriro chake ndichofoka ndipo akuyetsa Mulungu ndi chikopa cha mame. Oweruza 6:36-40.

C. Gideon tsopano wakonzeka kutsogolera asilikali a Mulungu. Mutu 6:1-18 akunena momwe Mulungu adakonzekeretsa asilikali ache. Tikuona kuti Mulungu adabwedza anthu onse ndikungotsiya anthu okwana 300 ngati asilikali chifukwa Mulungu amafuna kuonetsa kuti simphamvu za anthu koma ndi mphamvu za Mulungu zomwe zimapereka chipambano.

D. Asilikali 300 adakumana ndi asilikali okwana 135 000 ndipo Mulungu adapangitsa iwo kusalaza khamu la nkhondo la Amidiyani. Oweruza 7:19-25 akulongosola monveka bwino kuti Mulungu adapambana osati anthu.

Yefita adali oweruza woipa onani mutu 11:1-12:7. Onani nkhani ya chowinda chake (11:29-40).

A.Kodi chowinda chakechi chidali chabwino vesi 30-31? Ndithu chidali chowinda choipa. Onani zotsatira za chiwinda chake vesi 34-40. Mukuganiza kuti Mulungu amafuna munthu kupereka mwana wake nsembe? Levitiko 20:1-4 Mulungu akuletsa mchitidwewu kolimba zedi. Phunziro kwa ife ndilakuti tizipanga zowinda zomwe zili zotsangalatsa Mulungu.

III. Bukuli likumaliza ndi nkhani zoopsa ziwiri za kusasunga kwa chilamuli ndi kulimbana kwa pachiweniweni.

1. Gawo lotsiridza likutsiyana ndi gawo loyamba-mavuto a mkati ndilimene lidali vuto lalikuru kutsiyana ndi poyamba pamene mavuto amachokera kunja kwa adani awo. Israyeli adali m'dani wa iye mwini monga momwe ulili mpingo lero. Kulimbana kuli mkatikati mwa mpingo. Ili ndi vuto lomwe mpingo wathu ukukumana nawo lero.

A.Mutu 17-18 akunena za nkhani ya Mika; nkhani ya kupembeza mafano yomwe imachitika pakati pa Alevi ndi Adani. Ndichimodzimodzi ndi abusa anu pamene alambira mafano.

B.Mutu 19-21 ukunena nkhani yonvetsa chisoni yakugwirira ndi kupha bwenzi la mlevi ndi anthu a mfuko la Benjamini. Izi zidayambitsa nkhondo pakati pa Abenjamini ndi mtundu wonse wa ana a Israyeli. Zikungoonetsa kugwa kotheratu kwa anthu osankhidwa a Mulungu-kutsika kufika pa mulingo wa anthu aku Sodomu ndi Gomora.

2. Oweruza 21:25. Mfumdo yakuti m'mbuyomo mudalibe mfumu koma aliyense amachita choyenera m'maso mwa onse zikutiphunzitsa kuti tikuyenera kusunga ndi kusogozedwa ndi Malamulo ndipo tikuyenera kutsiyanitsa chabwino ndi choyipa. Mulungu amatipatsa Malamulo kuchokera m'Baibulo.

RUTE-Limodzi mwa mabuku awiri amene ali ndi mayina a azimayi

Iyi ndi nkhani yotsangalatsa ya dalitso la Mulungu kwa anthu okhulupirika mwa njira yopatulika. Tikuona pa mutu 1 kuti nkhaniyi idachitika munthawi ya Oweruza.

Rute, Naomi ndi Boazi ndi atenga mbali akuluakulu munkhaniyi. Rute si muhebri koma ndi mpongozi wake wa Naomi. Ndi akazi awiri amasiye-osauka ngati aku Malawi, Rute amakonda apongozi akewa ndipo adabwerera limodzi ku Israyeli. Boazi

adapalana ubwenzi ndi Rute ndipo pamapeto pake adalowa m'banja. Adachita moyenera kwa Boazi kutenga Rute muukwati motsatira Malamulo. Rute ndi Boazi ndi agogo ake a Davide ndipo mu mibadwo ya Ambuye Yesu muli Rahabu amene adali hule.

Bukuli likubwera mosatana ndi buku la Oweruza zomwe zikuonetsa kusakhulupirika kwa ana a Israyeli munthawi ya oweruza, ndimomwe ana a Israyeli adalangidwira chifukwa chakusanvera kwao. Rute akutiuza za mphoto yomwe Mulungu adapereka kwa anthu atatu okhulupirika. Rute adali wa ku Moabu, ndipo nkhaniyi ikutsimikidzira kuti pangano la Mulungu silili la ntundu umodzi wa anthu koma ngakhale enanso amene amatsangalala ndi phindu la kukhala amodzi mwa anthu a Mulungu; okhala mu pangano la Mulungu.

1. Rute mutu 1 akunena kuti Rute ndi apongozi ake adataya amuna awo ndipo onse awiri adakhala amasiye ku Moabu kwao kwa Rute. Naome adabwerera kwao ku Israyeli ndipo Rute adapita naye limodzi.

2. Rute pa Mutu 2 akukumana ndi Boazi amene akumuchitira chifundo.

3. Rute ndi Boazi akwatirana (mutu 3-4) ndipo ndi agogo a mfumu Davide zomwe zikupangitsa kuti akhale mu m'ndandanda wa makolo a Yesu Khristu (Mateyu 1:5-6 ndi 36).

I ndi II Samueli

Samueli, Sauli ndi Davide ndi atenge mbali akuluakuluru mubukuli. Samueli ndi munthu weniweni wa Mulungu. Palibe cholakwika chilichonse chomwe tikuchimva mumbiri yake kutsiyana ndi anthu ena amene ali m'Baibulo monga mfumu Davide.

I Samueli

1. Ngakhale kubadwa kwake kukupereka phunziro kwa ife. 1Samueli 1:1-8 tikunva za Hana yemwe adakwatiwa kwa mwamuna yemwe adali wamitala. Hana adali osabereka ndipo amakhumba atakhala ndi mwana. Adanyozedwa kwambiri ndi mkazi nzakeyo amene adali kubereka ana (1 Samueli 6).

2. Hana adatembenukira kwa Mulungu (vesi 9-18) ndipo adapempherera mwana kuchokera pansi pa mtima wake ndikulonjeza kwa Mulungu kuti akamupatsa mwana, mwanayo azamupereka ku utumiki wa Mulungu m'moyo wake onse. Onani vesi 18 akunena za ntendere wa mu mtima womwe Hana adali nawo atangomaliza pempheroli ndipo adapereka zopempha zake kwa Mulungu. Adawinda kwa Mulungu kuti mwanayo azakhala nazili. Kodi ichi ndi chowinda choyenera? Kumbukirani chowinda cha Yefita? Pa Luka 1 Mzimu Woyera udalamula kuti Yohane M'batizi azakhala mnaziri. Timanva za Naziri koyamba kuchokera m'buku la Numeri 6:2-8 ichi ndi chowinda cha kupatula khaya m'moyo kapena munthawi yochepa.

3. Mutu 1:20 tikunva kuti Mulungu adamupatsa Hana mwana wamwamuna ndipo adasunga lonjezo lopereka mwanayu ku utumiki wa Mulungu. Pamene Samueli adangoleka kuyamwa adapita kukatumikira Mulungu pamodzi ndi wansembe Eli. Hana mwaufulu adataya chimwemwe cholera mwana wake pamene adampereka iye kwa

Mulungu. Kawirikawiri kutumikira Mulungu kumakhala ndi dipo loti tipereke. Mwachisanzo mamishonare amatsiya mawanja awo.

A. Kumbukirani mau a Yesu kuchokera pa Marko 8:34 “ndipo anadziitanira khamulo la anthu pamodzi ndi ophunzira ake, nati kwa iwo, ngati munthu afuna kuza pambuyo panga, adzikanize yekha, nanyamule mtanda wake, nanditsate Ine.” Anthu a Mulungu amaitanidwa kuti zipereke okha nsembe.

4.Nyimbo ya Hana (mutu 2:1-11) iye adalambira Mulungu. Izi zitha kuyerekezedwa ndi pemphero la Mariya ndi anthu ena omwe adalemekeza Mulungu chifukwa cha kukhulupirirka kwake. Tikuyenera kutengera zimenezi potaya nthawi yathu yochuluka ndikulemekeza Mulungu.

5.Mutu 2-3 tikunvamo za kuipa kwa ana a Eli ndi chiweruzo chomwe adapereka—chomwe idali imfa ya banja lonse la Eli yomwe idachitika patsogolo pake imene ikufotokozedwa pa 1Mafumu 2:27.

6.Mutu 3:1-10 ukunena zokhuzana ndi kuitanidwa kwa Samueli komanso momwe Mulungu adakhalira ndi iye. Samueli adali Oweruza wotsilidza. Tiyeni tikambirane za maitanidwe a Mulungu.

7. Mutu 4:10-11 tikunva za kulandidwa kwa Likasa. Likasali lidali chinthu chofunikira kwambiri ndipo limayimirira kupedzeka kwa Mulungu. likasali lidapita chifukwa amaligwiritsa ntchito molakwika, politenga kunkhondo kuti likapereke mwayi opambana, kapena amalitenga ngati chifaniziro cha Mulungu popita nalo kunkhondoko. Tikambe za zifaniziro zonga izi masiku a lerowa—maula kapena kuvala ntanda ndi mankhwala a mwayi lero.

8. Mutu 8 Israyeli akuvuta chifukwa akufuna kuti akhale ndi mfumu. Tiuona kuti ana a Samueli adaikidwa kuti akhale oweruza mmalo mwa bamboo awo, koma ana ake adali oyipa chifukwa amakonda kulandira ziphuphu. Izi zidapangitsa akulu a anthu kukana anawa kuti akhale oweruza ndikukakamidza kuti akhale ndi mfumu. Samueli adali ozunguzika, koma Mulungu adamuuza kuti sakukana iye koma akukana Mulungu (vesi 7). Mulungu kudzera mwa Samueli adauza anthuwa mavuto obwera chifukwa chakukhala ndi mfumu (Mutu 8:10-18). Vesi 19-22 tikunva zoti Mulungu adapereka kwa anthu chopempha chao. Pamene tikuona mavuto obwera chifukwa chokhala ndi mfumu tidzaona choona cha chenjezo la Mulungu. anthu amayetsera kutsata mfumu yao ndipo mfumu yoipa imatsogorera anthu kukhala pamavuto ndi Mulungu.

9. Mutu 9 tikuona Mulungu akusankha Sauli kuchokera ku mtundu wa Benjamini kuti akhale mfumu. Onani pa vesi 2 kuti muone kufotokozeredwa kwa maonekedwe a Sauli. Kumbukirani zomwezi pamene tidzakhale tikuyang’ana nkhani ya Davide.

II. Nkhani ya mfumu Sauli Davide asadalowe ufumu. Tikuona mtundu wa ufumu wa Sauli.

1. Mutu 10 akunena za kuzozedwa kwa Sauli amene amachokera mu fuko la Benjamini.

2. Samueli adatula udindo wake ngati ntsogoleri mu chaputala cha 12 ndikulimbikitsa anthu kuti amvere Mulungu. Vesi 13-15 akulankhula monga mwa malangizo osiliza a Mose kwa anthu ake.

3. Patangopita kanthawi kochepa ndi kupambana kowerengeka, Sauli adaulula poyera mtima wake weniweni. Mutu 13:8-14 tikunva za Sauli kuti adapereka nsembe kwa Mulungu zinthu zomwe Samueli adamudzudzula pakuchita izi. Ndichifukwa chani kudali kosayenera kuti sauli apereke nsembe? Izi zidapangitsa Samueli kumuuza Sauli kuti ufumu wake suzapitirira ndipo kuti Mulungu waganiza zosankha mfumu wina—mfumu ya pamtima pa Mulungu.

4. Mutu 13-14 tikunva kupitirira kwa chipambano chomwe Sauli amakhala nacho ngakhale amapanga ziganizo zolakwika monga kuthamanga kuwinda ponena kuti pasapezeke wina aliyense wotenga chakudya asadagonjetse

5.Mutu 15 ukunena za kukanidwa kwa Sauli ngati mfumu maulendo awiri. Sauli adalangizidwa ndi Samueli kuti akaononge adani onse ngakhale ndiziweto zawo zomwe. Ndipo Sauli sadanvere zolamulidwa ndi Mulunguzi, ndipo Mulungu adamuuza Samueli kuti ali ndi chisoni chifukwa adamuika Sauli kuti akhale mfumu. Sauli akubwera molapa koma akuchita izi zinthu zitaonongeka kale, kotero Samueli akumuleka kwa muyaya.

III. I Samueli 16-31 akunena za mfumu Davide ndi mfumu Sauli. Sitingathe kukamba zonse mwasatanesatane, kotero ndingokupasani nkhaniyi mwachidule. Mulungu adatenga Davide kuti akhale mfumu yachiwiri. Onani zomuyenereza zake muchaputala 16:7, kwambiri homuyeneredza chake udali mzimu wake. Ndikwabwino kuweruza munthu chifukwa cha mtima wake monga Mulungu amachitira (Luka 11:39 ndi Mateyu 23:27).

1. Muli nkhani yaitali m'buku la Samueli yomwe yayenda mpaka kumapeto kwa bukuli. Nkhaniyi ikunena za Nsanje ya Sauli amene nthawi zonse ankayetsetsa kuti amuphe Davide chifukwa cha nsanjeyo, ngakhale Davide adali ndi mwayi ovulaza Sauli koma adakana kupha Sauli amene iye amamutenga ngati ozozedwa wa Yehova. Tiona nkhani zotsatirana zimenezi.

2. Mutu 17 tikuona nkhani yotchuka ya Davide ndi Goliyati. Nkhaniyi imatiuza za chikhulupiriro chachikuru cha Davide amene adakhulupirira Mulungu ndi moyo wake, kotero Davide adapambana ndi chipambano cholimba pamodzi ndi mfumu Sauli.

3. Mutu 18:1-16 tikunva za nkhani ya kuyamika kwa Mtima wa Sauli pazomwe Davide adachita, koma posakhalitsa Sauli adayamba kumuda Davide ndipo adayetsetsa kumupha iye. 1Samueli 18:7-9 akutionetsa chimene chidayambitsa mkwiyo wa Sauli kuti achite Nsanje kwa Davide. Nsanje imaononga anthu ambiri.

4. Tikuona pa mutu 18:10 kuti Mulungu adatumiza mzimu woyipa mwa Sauli, omwe udatsintha Sauli kukhala munthu wamisala. Tebwererani m'mbuyomu ndikuona chaputala 16:13-14. Tikuona kuti Mulungu walanda madalitso ake kwa Sauli ndikupatsa awa kwa Davide.

5. Vesi 11 ikunena kuti mkwiyo wa Sauli udakula mpaka adafunanso kupha Davide, koma monga tikuonera Mulungu adapereka madalitso ake kwa Davide, kotero ngakhale Sauli adayetsera kupha Davide mobwerezabwereza, koma sakadakwanitsa kulaka madalitso omwe adali mwa Davide.

6. Mutu 17:1-7 Davide akadatha kupha Sauli, koma tikuona chifukwa chomwe sadachitire izi. Davide amakonda ndi kunvera Mulungu ngakhale izi zikadatanthaudza kuti Sauli akadakhala akusakasaka moyo wa Davide.

7. Davide adapirira kwa zaka zambiri akusakidwasakidwa ndi Sauli, koma sadamuvulaze iye chifukwa amanva nkati mwake kuti "Sauli adali ozozedwa wa Mulungu." Mutu 1 wa Samueli wachiwiri akunena kuti Davide adalamulira kuti afe munthu amene adapha Sauli.

8. Mutu 29 ukunena za kuipa ndi kukhala kutali ndi Mulungu m'moyo wa Sauli, pamene adapita kukaombedza maula. Deutronomo 18:10-12 akuletsa zomwe Sauli adachita. I Mbiri 10:13-14 akutiuza kuti izi zidapangitsa imfa ndi mathero a banja lachifumu.

II Samueli

Iyi ndi nkhani ya ufumu ndi kulamulira kwa Davide. Amadziwika kuti adali munthu yemwe adachita zinthu zambiri zoipa, komanso amadziwika kuti ndi munthu amene adakondedwa ndi Ambuye, chifukwa nthawi zonse amalapa mwa change akalakwitsa. Choyamba amadziwika kuti m'gonjesi. Amamenya nkhondo mowirikiza ndikukulitsa malire poyenjedzera malo amene Mulungu adalonjeza kwa ana a Israyeli. Choyamba Davide adalimbitsa Yuda kenako adalimbitsa Israyeli yense. Nkhondo zomwe amamenya kumapeto kwa moyo wake zimachitika chifukwa cha tchimo lomwe adachi ndi Betiseba, lomwe lidapangitsa mwana wake m'ntsogolo mwake awukire bamboo akewa.

I.Gawo loyamba mutu 1-10 ukunena za nkhondo zoyamba za Davide zomwe amazimenya pofuna kulimbitsa ufumu wake.

1.Zidamutengera zaka 6 kuti Davide akhazikitse ufumu wake. Pamodzi Davide adalamulira zaka 7 ndi theka ndi ndipo adalamulira Israyeli yense kwa zaka 33.

2. Mutu 5 akunena momwe asilikali ake adagonjetsera Yerusalemu, yemwe amatchedwanso Zioni, komanso mzinda wa Davide. Uwu udasandulika likuru la dziko la Israyeli komanso paphata pa mapemphero. Mpaka lero mzindawu ndi likuru.

3.Mutu 6 ukulongotsola momwe Likasa la Mulungu lidakalowera ku Yerusalemu. Vesi 6-7 akutikumbutsa ife kuti Mulungu amayenera kuti azinveredwa. Mavesiwa akuulula kulakwitsa kuwiri. Choyamba sadayendetse likasali monga momwe Mulungu adalamulira.—onani Exodo 25:12-14. Komanso Uzza samayenera kugwira likasali chifukwa sadali M'levi. Iyi ndi nkhani yozunguza maganizo, koma izi zingotithandidza kudziwa kuikapo mtima kwa Mulungu kuti tisatire zomwe akuzilamulira komanso kutionetsa kuti samasekerera tchimo.

A. Davide pamodzi ndi anthu onse adakondwa kuti likasa lapita ku Yerusalemu (2Samueli 6:13-21). 2 Samueli 13-15 akunena za chisangalalo chopambana. Ndikwabwino kukondwerera Mulungu.

B. onani vesi 16, 20-23 pamene Mikala mkazi wa Davide anadandaula mwamuna wake m'mene adasangalalira. Kumbukirani kuti adali mwana wa Sauli. Mukuganizapo chani pazimenezi?

4.Mutu 7 Davide adakhumba poyamika Mulungu kuti amange malo opembedzera Mulungu, koma Mulungu adakana. Kenako mubuku la 1Mbiri 22:8 timawerenga kuti idali ntchito ya mwana wa Davide kumanga malo opembedzera chifukwa Davide ali ndi mwazi wochuluka muzanja lake. Mulungu adapereka mphoto pankhalidwe la Davide ndipo adapangana pangano ndi Mulungu ndipo adamuuza kuti;

A. Vesi 10-11 Mulungu adzapereka malo otetezeka kwa Israyeli kuti adzakhaleko kwamuyaya.

B. Vesi 12-13 Mulungu adzautsa mwana wa Davide kuti amumangire kachisi.

C. Vesi 13 Mulungu adzakhadzikitsa ufumu wa Davide kwa muyaya.

D. Vesi 14 Mulungu adzakhazikitsa ubale wa mwana—atate ndi ana a Davide. Timasangalala ndi ubale umenewu lero popedza ife timayetsedwa ana a Mulungu.

E. Vesi 14-15 chikondi chopotsa cha Mulungu sichidzachoka mu ufumu wa Davide kutsiyana ndi Sauli. Ili limadziwika ngati Pangano la Davide lomwe limakwaniritsidwa mwa Yesu.

Vesi 18-19 tikuonamo pemphero la chiyamiko la Davide.

5.Mutu 8-10 tikuonamo chipambano chachikuru komanso ntchito ya chifundo kwa chizukuru cha Sauli.

II. Mutu 11-19:8 tionamo za tchimo la Davide komanso mavuto a m'banja mwake

1. Zabwino zonse zili m'mbuyomu zikusogozana ndi ndi nkhani yoipa ya tchimo la Davide lakupha ndi chigololo. Mutu 11 akunena za chigololo pakati pa Davide ndi Betiseba zomwe zidazetsa imfa ya mwamuna wa Betiseba pamene mkaziyu adadziwika kuti ali ndi pakati. Kotero mfumu Davide adachita tchimo la chigololo ndi tchimo la kupha.

2. Mutu 12 tikuona momwe mneneri Natani adamfikira Davide ndi tchimo lakeli ndipo vesi 13 ikuulura mtima wa Davide, chifukwa pamene chilango chidayankhulidwa Davide mofulumira adalapa. Vesi 15-22 akunena za kumwalira kwa mwana wa pakati pa Davide ndi Betiseba. Davide adasala ndikupemphera kuti mwanayo asafe, koma mapeto ake mwanayu adamwalira. Timaphunzira kuti tchimo la Davide lidakhululukidwa koma adalangidwa. Vesi 23 ikutiudza kuti kuli moyo kuseli kwa imfa ya moyo uno. Tikuona kuvomerezedwa kwa Davide muchifuniro chake cha Mulungu.

3. Mutu 13-18 akupitilidza kuonetsa dipo lomwe Davide adapereka chifukwa cha tchimo lomwe adachita; mwana wake Amunoni anagwirira mlonga wake Tamala zomwe zidapangitsa Abisalomu kuti aphe m'chimwene wakeyu. Izi zidazetsa kuukira kwakukuru kwa Abisalomu pamene amakakamiza bambo ake kuti achoke munzindawu. Abisalomu mosabisa amachita za chiwerewere ndi akazi a bambo. Pamapeto pake Abisalomu adaphedwa, ndipo mosabisa Davide adalira maliro a mwana wake Abisalomu. Munthu atha kulapa koma Mulungu amamulanga padziko lapansili chifukwa cha tchimo lake.

III. Mutu 19-24 ndimathero omwe akunenabe za mavuto a Davide.

1. Mutu 20 ukunena za munthu opanda pake dzina lake Seba amene adatsogolera kuchitira upandu mfumu Davide.

2. Mutu 21 ukuyamba ndikutiudza zokhuzana ndi njala ya zaka zitatu yomwe Mulungu akunena kwa Davide kuti gwero lake ndi chisalungamo chimene chidachitika ku fuko la Agideon ndi Sauli. Adavomeredza kunyongedwa kwa ana 7 a Sauli kuti athese vutoli.

3.Mutu 21 chikutsiriza chikukamba za nkhondo ina ndi Afilisti.

4.Mutu 22 tikunva za Nyimbo ya Davide ya chiombolo. Werengani vesi 1-7.

5.Mutu 24 ndiomwe ukutsiliza buku la II Samueli ndi nkhani ya Davide atagwanso kawiri mumavuto. Tikuwerengamonso zokhudzana ndi kugulidwa kwa malo mu Yerusalemu ndi cholinga choti adziperekerapo nsembe zopsereza za kwa Mulungu. muli zabwino ndi zoipa mu chaputala chotsilidzachi molingana ndimomwe Davide adalamulira moyo wake.

A. tikuwerenga muvesi 1 pamene Mulungu alola Satana kulamulira moyo wa Davide kuchititsa kalembera zomwe zili zosemphana ndi Malamulo a Mulungu.

B. sitikuziwa chifukwa cha kulakwika kwa chiganizochi, koma vesi 10 ikuonetsa kuti Davide adadziwa kuti kulakwa polamulira kalembera, kotero chikumbumtima chake chimamutsutsa, kotero adaita machawi kuti alape.

C. Vesi 11-17 ndi nkhani ya momwe Mulungu adalangira Davide. Adamupatsa chisankho pa zilango zitatu. Davide adasankha kotero Mulungu adaumiza nthenda yomwe idapha anthu okwana 70,000. Chenjezo la Samueli mu 1 Samueli 18:9-18 lidali lolondola kuti mafumu amayambitsa mavuto. Ndani akufuna mfumu?

E. 2 Samueli 24:18-25ndi nkhani yomaliza mubukuli yomwe ikunena za Davide amene adagula malo ndikumangapo guwa la nsembe, awa adali malo omwe pamapeto pake padamangidwa kachisi. Vesi 24 pali phunziro kwa ife kuti tikhale ndi chikhumbokhumbo chopereka dipo kuti titumikire Mulungu. tikudziwa kuti zikwi za akhristu padziko lonse akuphedwa kapena kuzunzidwa chifukwa pano chifukwa akutumikira ndi kupembedza Mulungu m'maiko ambiri pano padziko lapansi.

Pansipa pali nkhani yokhudzana ndi mazunzo a akhristu ya ku Uganda.

Kuzunzidwa kwa akhristu matsiku ano kwambiri kukuchitika kumaiko amene Chisilamu ndi chokula mphamvu. Idi Amin amene amazitcha kuti ndi Pulezidenti wa muyaya, amene adali m'silamu adatenga ulamuliro wa dzikolo muchaka cha 1971 ndipo adayetsera kutsintha Uganda kuti likhale dziko la chisilamu ndi chithandizo chochokera kwa Aluya komanso ku Libya.

Koma vuto lomwe adakumana nalo lidali lakuti anthu ambiri adali akhristu alimbika kwambiri, kotero adayamba mchitidwe amene adali ndi chikhulupiriro chopotsa….. pakutha pa zaka za ulamuliro wake wauchigawenga mu 1979 pamene adagwetsedwa ndi asilikali a ku Tanzania, anthu okwana 500, 000 adali ataphedwa, ndipo 300, 000 mwa anthuwa adali akhristu

Akhristu tikhale okonzeka kulipira dipo, pachikhristu chathu.

I ndi II Mafumu

Monga mutu wake ukunenera, iyi ndi nkhani ya mafumu onse pambuyo pa mfumu Davide kufikira nthawi ya kugwa kwa Yerusalemu ndi mathero a ulamuliro wa eni

dziko. Ndinkhani yachisoni kuti Solomoni adakhalapo mfumu panthawi imene Israyeli adali olemera ndi wamphamvu. Kwambiri ndi nkhani ya kulephera kwa anthu a Mulungu kuti anvere Mulungu, zomwe zidapangitsa kugwa pansi kofulumira kwa dziko lawo. Mfumu Solomoni idalowa paudindo ndi chiyembekezo chachikuru, koma kudapedzekanso kuti adakwatira azimayi achikunja zomwe zidapangitsa kuti agwe mu nsampha wa kupembeza mafano a akaziwa. Buku la Mbiri likubwereza nkhani za ufumu wa Israyeli, koma zikutsiyana popedza bukuli likukambanso za ansembe.

Tizagawa Mafumu oyamba m'magawo awiri. Gawo loyamba, Mutu 1-12 tikunva nkhani ya Solomoni ndi dziko la Israyeli lisanagawikane, ndipo gawo lachiwiri likunena za mbali yoyamba ya ufumu ogawanika. Mabuku awiri amafumu ndi buku limodzi lokha, ndipo nkhani ikungopitirira kuchokera mu buku loyamba kupita mu buku lachiwiri. Ndi nkhani ya anthu a Mulungu omwe atchera Mulungu misana ndikusata milungu, ngakhale Mulungu wayetsera njira zambiri zobwedzera anthuwa kwa Iye mwini wake. Kufikira kuti amatumiza aneneri.

I. Mfumu Solomoni alamulira Ufumu osagawanikana.

1.Mutu 1:1-5. Kuyambira Davide asadamwalire, padali banja lomwe limalimbalimba kufuna ufumu. Adonija mwana wa ana a akazi a Davide oyamba, adaziika yekha mfumu, ndi ulamuliro wayekha, omwenso adalibe. Pamene Davide adanva izi adalengeza kuti Solomoni mwana wa Betiseba azakhala mfumu. Kumapeto kwake Adonija adaphedwa, ndipo Solomoni adalimbikitsa ufumu wake popha mchimwene wake wabere lina.

2. M'mutu 2:1-4 tikuona mau osiriza a Davide kwa Solomoni, amene adamulimbikitsa mwana wake kuti akhale okhulupirirka pamaso pa Mulungu. tikuona malonjezo a madalitso pakunvera mauwa.

3. Mutu 3 akunena mu vesi 1-2 kuti mbeu ya kugwa kwa Israyeli ikudzalidwa pamene Solomo adalowa mupangano ndi Farao kuti akwatire mwana wake. Chotsatira tikuwerenga za cholinga chachikuru cha ulamuliro wa Solomo. Vesi 5-14 akunena momwe Mulungu adafunsira Solomo chomwe akufuna, ndipo m'malo mopempha zinthu za iye yekha, Solomo adapempha nzeru kwa Mulungu, kuti akhale ntsogoleri wabwino. Izi zidasangalatsa kwambiri Mulungu, ndipo adamuyenjezera zinthu zina pamwamba pa nzeru, werengani vesi 12-14. Vesi 16-28 akunena za chiganizo chomwe chidaonetsa kuti Solomo adalidi ndi nzeru.tikuona kuti Solomo adayambadi ngati mfumu yaikuru, koma tiona kuti kusakhulupirika kwake pamaso pa Mulungu, kudamupangitsa kugwa ndikusakhalanso mfumu yaikuru.

4. Mutu 4 akunena za kulemera kwa ufumuwu chifukwa cha dalitso la Mulungu lomwe lidali pakati pawo. Vesi 20-23 ndi 25-26. Onani vesi 29-31 kuti mutsimikidze za Solomo odala.

5. Nkhani yotsatira ndi madalitso ena; kumanga kwa kachisi komwe kukuyamba m'mutu wa 5 kufikira kuperekedwa kwa kachisiyu mu chaputala cha 8. Kachisi adakhala malo amene Mulungu amakumana ndi anthu ake, kumene amakalambirako Mulungu. kachisi adali wantengo wapatali komanso okongola m'mamangidwe ake. Mwachitsanzo, padali golide ochuluka amene adagwiritsidwa ntchito pomanga kachisiyu. Kachisi adamangidwa zaka za chipambano cha ufumu wa Solomo. Onani mu

vesi 63 ya chaputala 8, kuti mutsimize zochuluka zimene zidaonongedwa popereka kachisiyu. Kwazaka mazana moyo wa Ayuda umasamira kwambiri pa kachisi. Koma tsopano alibe malo kukaperekapo nsembe ya chikhululukiro cha machimo awo.

6. mutu 9:1-9 tikunva kuti kachisi atangotha, Mulungu kachiwiri adaonekeranso kwa Solomo. Mulungu adabwerezanso lonjezo la madalitso pakunvera kwao ndi chilango choopsa pakusanvera kwao.

7. mutu 9:10-11:13 akulongosola za zaka zaulemerero za ufumu wa Solomo. Anadalitsidwa ndi chuma chopotsa mafumu ena. Mafumu ena amamulemekedza iye. Tikuonanso kuti adali akazi achikunja okwana 700 ndi mabwenzi okwana 300. Mutu 11:2-8 tikunva kukwiya kwa Mulungu chifukwa cha izi, ndipo akaziwa adamupangitsa Solomoni kuyamba kupembedza mafano m'malo mwa Mulungu wakumwamba.

8. Mutu 11:9-13 akunena tchutchutchu chifukwa chimene Mulungu wakwiya ndi Solomo, ndipo chilango chake ndichakuti Mulungu azutsa m'dani wake wa Solomo, Yeroboamu amene adzatenge mbali yaikuru ya ufumuwo kupotsa mwana wake. Mulungu adachedwetsa chilangochi kufikira Solomo atamwalira chifukwa cha Davide atate ake.

9. pali zoti tiphunzire kuchokera m'moyo wa Salomo. Solomo anadalitsidwa kupotsa munthu wina aliyense ndi nzeru komanso ndi chuma. Adali ndi chilichonse chomwe munthu akadachifuna chifukwa adali ndi Mulungu. koma pamapeto pake adamutsiya Mulungu, ndipo adazindikira kuipa kwa moyo wake. Werengani buku la Mlaliki, kuti mutsimikidze zoti Solomo adazindikira kuti adaononga moyo wake.

Anthu ambiri amadzindikira mochedwa kuti adakonda chuma ndikukhala muzikondwerero za moyo uno wa kuthupi, koma angoononga moyo wao. Tili ndi phukusi limodzi la moyo. Nfunso ndikumati, kodi tikhala m'moyo wozikondweretsa tokha kapena moyo wokondweretsa Mulungu?

Ulamuliro wa mfumu Solomo udali wosaiwalika mumbiri ya Israyeli. Timawerenga za kulemera ndi kukula kwa dzikoli. Koma Mbiri yoptsatira yonse ya Israyeli yangodzaza ndi kulephera ndi kugwa. Ufumu wa kumpoto udali wolephereratu, pamene ufumu wakumwera wa Ayuda umagwa kenako ndikudzukanso. Ufumu wa kumpoto udali ndi mafumu woipa okhaokha, pamene ufumu wa Ayuda, udali ndi mafumu ena ochepa amene amaopa Mulungu, amene amapangitsa kuti chilango cha Mulungu chichedwe kubwera.

II. Gawo lachiwiri la I Mafumu likunena za ufumu wogawanika.

1.mutu 12:4-14 olowa m'malo mwa Solomo adali mwana wake Rehoboamu, amene adali wankhaza ndi anthu ndipo adapangitsa anthu ambiri kuti amuukire. Nkhaza za Rehoboamu zidapangitsa kuti ufumuwo uwonongeke. Tikuwerenga vesi 18-19 ufumu wa kumpoto udagalukira. Iwo adapita ndi Yeroboamu nakakhadzikitsa ufumu wina kumpoto, wotchedwa ufumu wa kumpoto, kapena ufumu wa Israyeli, kapena wa Efraimu. Fuko lomwe lidatsala mu ufumu wakale ndi fuko la chiyuda ndi lina laling'ono la Benjamini.

2. choyamba chomwe Rehoboamu adachita ataona izi, kudali kutenga asilikali ankhondo, kuti akalande anthu ake, koma Mulungu adapereka uphungu wotsiyana ndi maganidzowa. Mutu 12:21-24. Ndichifukwa chiyani? Mwina Mulungu adachita ichi kuti apulumutse Yuda ku chipatsulo. Kumbukirani kuti Rehoboamu yemwe adali ndi mafuko awiri okha amafuna akalimbane ndi mafuko khumi a ufumu wa kumpoto. Timanva mumbiri kuti oatsogolo pake maufumu awiriwa adamenyana.

3.Mutu 12:25-33 mfumu Yeroboamu, adachita chinthu chomwe chidali ndi zosatira za nthawi yaitali mu Israyeli, adakhadzikitsa malo awiri opembedzerapo. Adapanga fano la ng'ombe ziwiri za golide kuti anthu ake azizilambira. Mwaichi adachotseratu anthu ake pamaso pa Mulungu, ndikuwalowetsa mu nchitidwe opembedza mafano. Adachita izi ndi cholinga choti anthu ache asapitenso ku Yerusalemu kukapembedza moyenera, komanso kukanyengedwa kuti alowe mu ufumu wa Chiyuda. Yeroboamu adali mfumu yoipa pamaso pa Mulungu. nthawi zonse Baibulo limanena za Mbiri ya mfumu iliyonse yatsopano ya Ayuda kapena a Israyeli, limanena ngati mfumuyo idali yabwino kapena yoipa pamaso pa Mulungu. mafumu onse a ku Israyeli adali oyipa; koma ena mwa mafumu a Chiyuda adali abwino, zomwe zikulongosola chifukwa chomwe chidapangitsa ufumu wa Ayuda kukhalapo nthawi yaitali kutsiyana ndi ufumu wa kumpoto.

4.Tsopno tiyeni tione za mfumu Ahabu yemwe tikuudzidwa kuti adali woyipa kutsiyana ndi mafumu amene adaliko asadakhale iye (1 Mafumu 16:30). Adakwatira mkazi woipa dzina lake Yezebeli, dzina lomwe limayerekedzedwa ndi uchimo matsiku ano. Tikuona mu vesi 31-33 chifukwa chomwe Ahabu amatengedwa kukhala oipa kupotsa mafumu okudza patsogolo pake, popeza adapangisa anthu a ku Israyeli kuyamba kulambira Baala. Vesi 33 ikunena kuti Ahabu adayetsetsa kuchita chomwe akadatha kuchita kuti akwiyitse Mulungu.

5.Mutu 17 tikuonamo za munthu wopotsa mBaibulo. Eliya akulowa m'bwalo maka mu ufumu wa Kumpoto. Mulungu amatumidza aneneri otsiyanatsiyana ku ufumu wa kumwera ndi kumpoto komwe. Ankachita izi kuti aneneriwa akonzetse khalidwe la anthu—powaitanira ku kulapa kwa machimo awo, ndikulambira komanso kutumikira Mulungu monga momwe ankadziwia.

A. chifukwa cha uchimo wa Israyeli, Eliya adanenera kuti sikuvumba mvula kufikira iye atazalora kuti mvula ibvumbe (mutu 17:1). Izi ndi zomwe zidachitika. Chidzindikiro cha mneneri woona, ndichimenechi kuti zomwe wanena zimachitika, ndipo vesi 7 ikutiudza kuti, chilala ndithu chinabweradi.

B. Izi zidapangitsa moyo wa Eliya kukhala pa chiopseza ndi Ahabu, kotero vesi 2-6 ikunena momwe Mulungu atetedzere ndi kusamalira mneneriyu. Tikuphunzira kuti ngati Mulungu ali mwa iwe, kuti umugwirire ntchito, Iye amakupatsa zosowa zako ndi kukutetedza.

C.vesi 7 ikutiudza kuti, idali nthawi pamene Mulungu adamuudza Eliya kuti apitirire nakagwire ntchito ina yomwe idali mmaganizo a Mulungu. vesi 8-24, mneneriyu adapita ku Zerafati kukapulumutsa moyo wa mkazi ndi mwana wake wamwamuna. Chinthu choyamba chomwe adachita kudali kuwapatsa chakudya, chifukwa adali pamavuto kaamba ka njala yomwe idali m'dzikomo. Kenako, malingana ndi mutu 17:17-23, tikunva kuti Eliya adadzutsa mwana kwa akufa. Zinali bwino kuti Eliya adachita izi kudziko la chilendo. Kenako mu buku la Luka 4:26 Yesu akunena za nkhani

imeneyi, pomanga nfundo yakuti, Yesu sadatumidwe kwa Ayuda okha, koma kupulumutsa anthu kuchokera m'maiko onse a dziko lapansi ku machimo awo. Ayuda adali akwiya ndi nkhani imeneyi, kotero adayetsera koyamba kuti aphe Yesu. Ndichifukwa chani Ayuda amachita Nsanje? Nsanje ndi tchimo loopsa kwambiri, lomwe limakhala ndi zotsatira zoopsanso, ndipo ili ndi vuto lalikuru ngakhalenso mu mpingo.

D. M'mutu 18 Eliya adabwerera ku Israyeli, komwe anthu akhala akuzunzika ndi chilala kwa zaka zitatu monga momwe Eliya adanenera matsikua a m'mbuyomo.

E. Mutu 18:23 pakuyambika imodzi mwa nkhani zomwe zimanditsangalatsa m'Baibulo; nkhani yobwino zedi. Nkhaniyi idachitika patatha zaka zitatu chineneri Eliya za chilala m'dzikoli. Eliya adaudza aneneneri a Baala kuti achite mpikisano ndikuona kuti amene akutumikira Mulungu woona ndi ndani. Werengani 20-39 nkhani yomwe Eliya adachepetsera aneneri a Baala. Onani momwe Eliya adatonzera aneneri a Baalawa mu vesi 27. Eliya adachititsa manyazi aneneri onyengawa, ndipo mu vesi 40 Eliya adapha aneneri onyengawa. Kodi mukukhulupirira kuti munthu angathe kuthamanga kuposa kavalo (vesi 46)? Zochitika izi zikuyenera kupangitsa anthu kukhala okhutitsidwa kuti ataye milungu yonama ndi kusata Mulungu woona komanso kumulambira Iye.

F. mutu 19 tikuona mantha amene anadza mwa Eliya amene anathawa mkwiyo wa Ahabu. Vesiyi ikutitsimikidzira kuti ife tonse imafika nthawi pamene chikhulupiriro chathu chimayamba kugwedera. Onani Mateyu 14:28-31 ndikuchitira umboni pamene Yesu anamuthandidza Petro kuti asagwe. Tikuwerenga vesi 5-16 tikuona Mulungu akutumikira Eliya pamene anatsautsika pamene anamubweretsera mphamvu kuti agwire ntchito yake. Vesi 18 ndi umboni kuti Mulungu amakhala ndi kagulu kotsala mwa ena otaika.

G. Mutu 19:16-21 tikuonamo za maitanidwe a munthu wina, yemwenso adali ofunikira, otchedwa Elisa mneneri amene adalowa mmalo mwa Eliya. Mulungu akuphunzitsa atsogoleri a mipingo kuti azikonzekera kuti utumiki wao udzakhale ukupitilira nthawi yao yokhala paudindo ikazatha. Ndikwabwino kuti atsogoleriwa aziphunzitsa wina wake amene kutsogoloko adzapitiridze utumikiwu. Ndili ndi chiyembekezo kuti utumiki womwe ndilimo lero, uzapitirira kwa nthawi yaitali ine ndikazamwalira

H. 2 Mafumu 2:1-12 akunena za kupita kwa Eliya kumwamba. Eliya ndi Enoki ndi anthu amene sadaone imfa kutengera ndi zomwe Baibulo limanena onani Genesis 5:24. Tikuwerenga kutumidzidwa kwa Gareta wa moto ndi Mulungu kuti azamutenge Eliya kupita naye kumwamba. Akhristu amene adzakhale moyo pakuweranso kwa Yesu kachiwiri, sadzaona imfa, onani 1 Atesalonika 4:16-17. Eliya ndi Enoki ndi anthu amene sadaone ululu wa imfa.

6.1 Mafumu akupitiridza kunena za kuipa kwa Ahabu ndi mkazi wakw Yezeberi. Tikuwerenga zimene adachita anthuwa kuba munda wa Naboti (mutu 21). Yezeberi mu vesi 9-10 adakonza kuti Naboti aphedwe kotero kuti abe munda wake mosavuta.

A. I Mafumu 21:17 akunena za Mulungu pamene adamutuma Eliya kuti apite kwa Ahabu ndikumuudza za machimo ake. Mu vesi 21-24 Eliya akulengedza za chilango

cha Ahabu ndi banja lake. Vesi 23 akunena za agalu kuti adzadya thupi la Yezeberi. 2 Mafumu 9:33-37 tikunvamo za kukwaniritsidwa kwa ulosiwu.

B. 1 Mafumu 21:27-29 akunena kuti chifukwa mfumu Ahabu anadzichepetsa, Mulungu adachedwetsa chilangochi kufikira m'badwo wotsatira. 2 Mbiri 33 akunenanso za nkhani yofanana ndi iyi, nkhani ya mfumu Manase. Mfumu Manase adali oyipa kwambiri mu Yuda, amenenso analapa pamene Mulungu analengeza chilango chomwe chingadze chifukwa cha uchimo wake, kotero Mulungu anachedwetsa chilangochi kufikira kumwalira kwa mfumuyu.

C. chotsilidza chomwe anachita Ahabu pamapeto pa zonse ndikusanvera mneneri, pamene analosera chipasuko kwa iye ngati angakakamire kupita kunkhondo. Kotero adamwalira chifukwa cha kusanvera Mulungu monga momwe amachitira m'moyo mwake.

7. monga Eliya, Elisa amachitanso chimodzimodzi poitana anthu kuti achoke ku mafano ndikupita kwa Mulungu woona, ndikukalandila madalitso ake.

A. Elisa nayenso adachita zozizwa zambiri (2 Mafumu 2 vesi 18-21) akunena za momwe adayeretsera madzi ku mzinda wa Yeriko.

B. Mutu 4:1-7 akunena zamomwe Elisa adathandidzira mkazi wamasiye wosauka. Ndemenga pa chikondi ndi chitsamaliro cha Mulungu kwa amai a masiye ndi ananso a masiye. Yakobo 1:27 akutiphunzitsa m'mene ife akhristu tingachitire ndi amai komanso ana a masiye—ndiopatulikanso pamaso pa Mulungu.

C. Mutu 4:8-36 tikunva kuti monga Eliya, Elisa adautsanso mwana wamwamuna. Pali anthu asanu amene anautsa akufa. Awa adali Eliya, Elisa, mu Chipangano Chakale, kenako Yesu, Petro ndi Paulo mu Chipangano Chakale.

D. Mutu 13 ukunena za imfa ya Elisa. Vesi 20-21 tikunva kuti angakhale anamwalira koma ndi mphamvu ya Mulungu m'manda momo amakwanitsa kuutsa anthu akufa. Zozizwazi zidachitika ndi Mulungu osati thupi lakufa la Elisa.

8. ntchito ya zozwizitsa ndi chiyani m'Baibulo, ntchito za chifundo? Kudali kulimbikitsa utumiki wa anthuwa monga Eliya ndi Yesu.

III. Chidule cha nkhani ya Israyeli—ufumu wa kumpoto.

1.kudali mafumu okwana 19 ku Israyeli amene adali woipa pamaso pa Mulungu. Ufumu wakumpoto udakhalako kwa zaka 208 asadatengedwe ukapolo, kenako udatengedwa ukapolo ndipo kuchokera pomwepo ufumuwu udathera pomwepo. Lidali kahlidwe logonjetsa mafumu munthawi imeneyo, ndikutenga anthu ogwidawo kupita nawo kudziko lakwawo, kenako kudzawabwedzera kwao. Izi amaganiza kuti amachepetsa kulimba kwa m'gwirizano kuti anthuwa atha kuukiranso. Amabwedza anthu ena kudziko lomwe awatenga.

Ayuda amene patsogolo pake adali anthu a munthawi ya Yesu Khristu anada Asamaliya amene amakhala ku malo a ufumu wa kompoto, omwe amaganiza kuti anawabera malo a abale awo. Muzawerenga za udani umenewu mu Chipangano

Chatsopano. Mafuko khumi amene adatengedwa ndi a Asuri sakunvekanso kuchokera nthawi imeneyo, ndipo amanenedwa kuti “Mafuko otaika a Israyeli.”

2. Nkhani ya mafumu a ku Israyeli ndi imodzi mwa nkhani zonvetsa chisoni kwambiri, popedza amatsiya Mulungu ndikutsata njira zawo zokhotakhota kufikira nthawi ya chilango chawo. Adachoka pa chuma ndi madalitso namira mu chipatsuko.

3. Tiyeni tione mfumu ina ya Israyeli yomwe idakhalako 815 B.C—mfumu Jehoahazi, werengani 2 Mafumu 13:1-9. Adali mfumu yoipa kwambiri, kotero Mulungu adalola adani ake kuti amulange iye. Pachifukwachi mfumuyi idapemphera kwa Mulungu, vesi 4, ndipo Yehova adawalanditsa iwo nakhalanso pantendere. Kenako vesi 6-7 akunena kuti anthuwa adachimwanso, ndipo Mulungu adabwerezanso kulanga ufumu wa nkuluyi. Mfumuyi adalamulira kwa zaka 17 asilikali a Asuri asadaononge asilikali ake. Kodi pali nfunso kuti ndichifukwa ninji Mulungu amalanga anthu ake? Tikuona phunziro lina apa lonena momwe utsogoleri wolakwika umapangitsira anthu kuti akumane ndi mavuto.

IV. Tione za Yuda. Ena mwa mafumu ake adali abwino pamene ena adali oyipa pamaso pa Mulungu. Mafumu abwino atha kukhala chifukwa chomwe chidapangitsa ufumu wa kumwera khalapo kwa nthawi yaitali.

1. 2Mafumu 18:1-8 akulongosola za mfumu Hezekiya kuti idali mfumu yomwe imalemekeza Mulungu. Iye adali mfumu pamene ufumu wa kumpoto udatengedwa ukapolo ndi a Asuri. Patapita zaka zochepa, chigonjetsere ufumu wa kumpoto, a Asuri adayambanso kulimbana ndi Yuda. Yuda yense adagonjetsedwa ndi a Asuri kungopatulapoYerusalemu.

2. Mutu 18:19-35 akunena za mwano omwe wankuru wa nkhondo adayankhula, kunyoza Yerusalemu ndi kuuza anthu onse kuti angozipereka okha, pamene asilikali awo adali atazungulira mzindawu.

3. Mutu 19 akunena za mantha a Hezekiya, amene adapita ku kachisi ndikukasanulira mtima wake kwa Mulungu, ndikupempha Mulungu kuti amupulumutse. Mneneri Yesaya adamuudza kuti Mulungu adzamupulumutsa, ndipo adalosera kuti a Asuri azabwerera kwawo atagonjetsedwa. Vesi 35-36 tikunva zakuphedwa kwa anthu okwana185,000 mwa asilikali a ku Asuri. Izi zidapangitsa a Asuri kubwerera ku dziko lakwawo ali ogonjetsedwa, ndipo ichi chidali chiyambi cha kutha kwa ufumuwu. Ndipo ufumu womwe udadzukanso ndi mphamvu padziko lonse udali wa ku Babulo.

4. Mfumu Hezekiya adamwalira ndipo mwana wake Manase adalowa m’malo mwake. Mutu 21:1-2 tikunva kuti motsiya ndi bambo ake Manase adali mfumu woipa kwambiri. Inali nthawi yake, pamene Mulungu adanena kuti azalola ufumu wake kuti utengedwe ukapolo monga zidachitira ndi ana a Israyeli (vesi 10-15). Kenako ali mu ukapolo, komanso akudzunzika, Manase adalapa ndipo Mulungu adalola kuti ufumu wake ukhalekobe kwa zaka zina zokwana 50.

5. Mutu 25 tikunva za momwe Babulo pansi pa mfumu Nebukadnezza adagonjetsera Yerusalemu, ndikutenga anthu kupita nawo ku ukapolo. Uku kudali kulangika kwakukulu, ndipo Ayuda ambiri adasauka ndi ukapolo. Mulungu amawapirira anthu,

koma pamene kupiriraku kwachepa mphamvu, kulanga kwake tsopano kumakhala kowawitsa ndi kotsapiririka.

1 ndi 2 Mbiri

1 ndi 2 Mbiri ndithudi ndi buku limodzi. Kwanthawi yoyamba pamene ndimawerenga bukuli, ndimadabwa ndi kubwerezedwa kwa nkhani zomwe ndaziwerenga kale. Ndizoona kuti bukuli likubwereza zambiri za zochitika za Ayuda, koma lalembedwa kuti likumbutse anthu za ubale wao ndi Mulungu. Mwanjira ina, bukuli lidalembedwa ndi maganizo okhudzana ndi chipembezo. Lidalembedwa anthu atabwera ku ukapolo, kumathero kwa nyengo ya mbiri ya Chipangano Chakale.

Munthu wina dzina lake Glaason Archer, adalemba kuti mabukuwa, “Adalongedwa ndi cholinga chachikuru, kuti apereka kwa Ayuda Chuma chosatha (Israyeli atabwera ku ukapolo) maziko enieni a uzimu a ulamuliro wao, monga anthu a pangano ndi Yehova. Cholinga cha anthu olemba mbiri ndikuonetsa kuti ulemerero woona wa Ahebri umapedzeka mu ubale wa Pangano ndi Mulungu.” Mulungu adawapatsa iwo mwayi wa Chiwiri.

M’mawu ena, mabuku a Mbiri ndi machenjezo onveka bwino, kuti Ahebri asatayenso kusonkhana mu kachisi, ndi kulambira Mulungu woona ndi wamoyo. Akhala akulangidwa molapitsa ndi Mulungu, kotero panopa akuyenera kuphunzira phunziro kuti akhale onvera Mulungu.

Ngakhale Ayuda anabwedzeretsedwa ku dziko lao, koma silidali dziko loima paokha monga momwe adalili mu nthawi ya Davide ndi Sauli. Amalamulilidwa ndi Aperisi ndipo ntsogolomo amalamulilidwa ndi Aroma maka munthawi ya Yesu. Kachisi yemwe adamanga adali onvetsa chisoni kutsiyana ndi yemwe adamangidwa ndi Solomo.

I. Ambiri mwa machaputala oyambirira, ndiokhudzana ndi mibadwo ya anthu; makolo a Ayuda kuphatikidzapo ndi iwo amene adachokera ku ukapolo. Ichi ndichifukwa chomwe chimatipangitsa kuti tidziwe kuti, mabuku a Mbiri adalembedwa anthu atabwera ku ukapolo.

II. Ambiri mwa mabuku a Mbiri ndizokhudzana ndi ulamuliro wa Davide ndi Solomo.

1. Mutu 10 akutiudza za kugwa paudindo kwa Sauli ngati mfumu. Vesi 13 akunena za kufa kwa mfumu Sauli. Chifukwa chidali chakuti adali osakhulupirika pamaso pa Mulungu, kufikira pa mulingo wakuti adayamba kufunsira thandizo kwa anyanga ndi amaula, m’mlalo mofunsira uphungu kwa Mulungu.

2. Mutu 11 ukuyamba nkhani yokhudzana mmene Davide adakhalira mfumu, kwa Israyeli onse ndipo timawerenga za mmene adali kulamulira dziko.

3. Mutu 16:8-17 tikunva za nyimbo yaikuru ya Davide ya chiyamiko ndi kuthokoza pamene amatsangala pamene likasa la Mulungu limapita ku Yerusalemu. Werengani ndi kugwiritsa ntchito nyimboyi pokutsogolerani mu mapemphero anu. Gwiritsani ntchito mau a Mulungu m’mapemphero anu.

4. Mutu 17 akubwereza lonjezo la Mulungu kwa Davide kuti ufumu wake udzakhala mpaka muyaya. (kodi ili limadziwika kuti ndipangano lanji? Longotsolani za ufumu womwe uzakhale kwa muyaya vesi 14? Ili limadziwika kuti pangano la Davide.

5. Davide sadaloledwe kuti amumangire Mulungu Nyumba, koma Mulungu adamulora kuti athandidzire kukonzekera kumangidwa kwa nyumbayi. Mutu 22 ndi 28 komanso 29 akunena zomwe adachita. Kwambiri iye adatorera zipangizo zoti zigwiritsidwe ntchito pomanga kachisiyu. Mutu 22:14 akutiudza momwe adatsonkhanitsira golide ndi siliva. Mutu 28 tikuona Davide akulangiza Solomo m'mene angamangire kachisi. Adapereka malangizo abwino kwa mwana wake, mu vesi 8-9 pamene amamulangiza kuti adziwe Mulungu ndi kumutumikira mokhulupirika. Malangizowa akubweranso kwa inu ndi ine.

6. Mutu 29 tikuona Davide kuti adautsanulira mtima wake pa Mulungu, pamene adapereka chuma chake chonse ku ntchito yomanga kachisi, chifukwa Davide adadzipereka ku kachisi wa Mulungu (vesi 3). Kenako mu vesi 6-9 tikuonanso kuti anthu mwaufulu adapereka zao ku ntchito ya kumanga Nyumba ya Mulungu, kotero adali okondwa pochita zinthu zimenezi. Taonani chitsanzo cha momwe mtima wathu ungakhalire ndi chuma chathu, ngati chinthu chofunikira kwambiri.

7. Mutu 29:10-19 ndi chitsanzo china cha momwe tingapempherere.

8. tili tsopano kumapeto kwa moyo wa Davide, ndipo dziwani kuti mulibe mmenemu chokamba chilichonse chokhudzana ndi tchimo lalikuru la Davide ndi Betiseba, kapena kuukira kwa Adonija. Nkhani ya mu 2 Mafumu 11:9-13 umunso siidaonetsedwe. Chidwi cha mabuku a Mbiri ndichabwino. Chidwi kwambiri ndi zokhudzana ndi Mbiri komanso chipulumutso. Olemba adawaudza anthu kuti ngakhale pambuyo pa tchimo lao lalikuru ndi chilango chomwe adachiona, koma pangano lidakhalabe logwira ntchito palibe chomwe chidataika.

III. Muli zochepa zokhudzana ndi ufumu wa kumpoto, mu Mbiri kwambiri akutsindika pa nkhani za kachisi komanso zina zabwino zokhudzana ndi ufumu wa Ayuda. Mulinso zambiri zokhudzana ndi kulambira Mulungu.

IV. Tsoka lotsiridza la Yerusalemu. 2 Mbiri 36.

1. Vesi 11-16 tikuona mfumu ya Ayuda ukulongotbsoledwa kuti ndi yoipa. Tikuonanso kuti atsogoleri onse a nsembe ndi anthu adali osakhulupirika. Chotsatira tikuona kuti popedza Mulungu adachitira chifundo anthu ake, adatumidza aneneri kuti awachenjedze, koma m'malo mwake anthuwa adanyoza machenjezowo, ndipo izi ndi chomodzimodzi kunyoza Mulungu.

2. Vesi 17-20 ikunena za chilango choopsa kupita kwa anthuwa. Amene adapulumuka pa nkhondo ya ku Yerusalemu, kupatula anthu osaukitsitsa adatengedwa kupita ku ukapolo ku Babulo (2Mafumu 25:12).

3. Chikondi cha Mulungu chikuonekera ngakhale pakulanga anthu ake, Mulungu akupereka tsogolo la chiyembekezo. Yeremiya adalonjeza (Yeremiya 35:11-12 ndi 29:10) kuti ukapolo uzatha pakazapita zaka 70. Kutsiyana ndi ufumu wa kumpoto, ukapolo wa Yuda sudali wamuyaya ayi.

4. Vesi 22-23 tikuonetsedwa za Koresi amene adasankhidwa ndi Mulungu, kuti apulumutse anthu. Werengani Yesaya 44:28-45:2 kuti muone ulosi onena za Koresi amene adaneneredwa zaka 100 izi zitsanachitike.

Ezara, Nehemiya ndi Estere

Mabukuwa akutsiridzitsa chigawo cha Mbiri ya Chipango Chakale. Buku la Estere lidalembedwa, anthu ali ku ukapolo, ndipo mabuku awiri otsalawo adalembedwa anthu atabwera ku ukapolo, komanso amaonetsa mmene anthu amakhalira mu Yerusalemu atabwera ku ukapolo. Apa tikuyembekedza kuona Ayuda atasintha khalidwe chifukwa cha phunziro lomwe aphunzira, ndikuti mokhulupirika azamvera ndi kupembedza Mulungu. Tiyeni tione mabukuwa ndikutsatira momwe zinthu zimachitikira mu Yerusalemu. Kubwera kwa anthu kuchokera ku ukapolo patatha zaka 70 kumakwaniritsa uneneri omwe tauona m'mbuyomu wa Yeremiya ndi Yesaya ndi Danieli.

Buku la Ezara kwambiri likufotokoza kubwerera kupita ku Yerusalemu kuchoka ku ukapolo.

1. Kubwerera koyamba kudachitika motsogozedwa ndi Zerubabelo mu 536 BC. Panali aneneri awiri amene adatumidzidwa ndi Mulungu munthawi ya ukapolo, ndipo ena atatu adakhalapo utatha ukapolo kuti atsogolere anthu. Mulungu samatsiye kutsogolera anthu ake.

2. Mutu 1 ukunena momwe Momwe Mulungu adamugwiritsira ntchito Koresi kuti alole anthu abwerera kwao ndikuwathandidzanso ndi zinthu zomwe amazifuna—onani vesi 1-8. Koresi sikuti pa umunthu adali ogawa ayi, koma idali ntchito ya Mulungu yomwe imachitika mwa iye.

3. Mutu 2 ukunena za omwe adabwerera ndi ntsogoreri Zerubabelo. Zerubabelo adali ndithu mbeu ya Davide. Ndi Ayuda ochepa amene anabwerera ku Israyeli.

4. Mutu 3 akunena kuti anthu adayamba kumanganso kachisi, koma nsuntso udaimitsa ntchitoyi mu 534 BC ndipo idayima kwa zaka 14. Choyamba adamanga guwa la nsembe kenako kachisi. Adayamba kumanga guwa la nsembe kuti kupereka nsembe kuyambenso.

A. zina mwa zifukwa zomwe zidaimitsa kumangidwa kwa kachisi ndi nsutso wa adani, koma tikuona chifukwa china m'buku la Hagai 1:4—anthu koyamba amalabadira za iwo okha. Tiyenera kutsiya Mulungu patsogolo, popanda apo sipadzapedzeka zochuluka kuti tikapereke kwa Mulungu—nthawi kapena ndalama.

5. Mutu 4:1-3tikuona adani a Ayuda akubwera kwa Zerubabelo, kukhala ngati akufuna kudzathandidzira ntchito, koma mwanzeru Ayuda adakana chithandidzo chawo, ndi kunvera ulamuliro wa Koresi. Pali zinthu zingapo zomwe tingaphunzire apa.

Choyamba ndichakuti pamene ntchito ya Mulungu ikupita chitsogolo, tiyembekedzere zobwedzeretsa m'mbuyo kuchokera kwa adani. Chinthu chachiwiri ndichakuti tisaphatikane ndi adani. Kodi m'dani ndi ndani? Amene si nkhristu kwa ife ndi m'dani chifukwa yense amene Sali nkhristu ali pa nkhondo ndi Mulungu; onani Aroma 5:10. Kotero onse amene amabwera kwa Zerubabelo kuti adzathandize sadali

abwenzi enieni. Adali ngati monga vesi 2 ikunenera kuti anthu amene amakhala mu Samaliya (ufumu wa kumpoto) adali anthu amene amapembedza milungu komanso mwa pang'ono pokha kulambirana Mulungu woona. Kusanganiza chipembezo cha chikunja ndi chikhristu sizingatipange ife kukhala akhristu enieni. Pali liwu lomwe limalongotsola za khalidwe lotchukali. Limatchedwa sencretism, kutanthaudza kuphatikidza zipembezo. Chitsanzo ndi kuphatikidza chikhristu ndi ufiti/nyanga, masenga. Chitsanzo china ndikulola munthu yemwe si nkhristu kulalikira mu mpingo wathu, monga anthu andale.

A. Ndikwabwino kudzindikira kuti akhristu akukhala kudziko lapansi, kotero tiyenera kukumana ndi dziko lapansi, koma tikuyenera kusamanga nalo ubale.

6. Adaniwa adaimitsa ntchitoyi kufikira nthawi imene mfumu ya tsopano ya Perisiya inakhala pa udindo. Mfumu Dariyo adalamula kuti kachisi amangidwe ndipo chuma cha mfumu chithandidzire ntchito yomanga kachisi. Mutu 6:8 . ntchito idayambikanso 520 BC ndipo idamalidzidwa kwa zaka zokwanira zinayi. Aneneri awiri Hagai ndi Zakariya adathandidzira kulimbikitsa anthu.

7. tiperekepo ndemenga pankhani ya momwe mfumu ya ku Perisiya idachita pothandidza Ayuda kuti akhadzikikenso mu Yerusalemu. Mafumuwa adali achikunja ndipo amadziwika ndi kumana ponena za ndalama zao. Koma tikuona kuti amapereka zambiri kuchokera ku chuma chao, kuthandidzira kumangidwanso kwa malinga a Yerusalemu ndi kachisi. Onani vesi 21-24 pa mutu 7 pamene tikuona mfumu akupereka ndalama, ndikuletsa ansembe ndi ogwira ntchito mmeneno, kupereka ntulo. Mulungu akuonetsa kuti akulamulira zonse zochitika padziko lapansi popangitsa anthu amenewa kukhala osamana. Nkhani za nsokhozi ndi mbali imodzi ya Malamulo a ku United States ku Amereca—machalichi asapereke nsonkho.

8. Mutu 7 akutiudza za Ezara amene akupedzeka mu vesi 6 ngati wansembe amene adali kadaulo pa nkhani za Malamulo ndipo amatsogolera ndi kulangidza anthu mu Yerusalemu za kupembedza Mulungu koyenera.

9. Tikuona pa Mutu 9 kuti anthu sadatengerepo phunziro, ndipo sanvera Mulungu. Ezara adasanulira moyo wake kwa Mulungu, mu limodzi mwa pemphero lake lalikuru m'Baibulo, werengani 9:2-15kuvomeredza machimo a anthu, ndikuzindikira kuti atsogoleri a anthu awatsogolera iwo ku uchimo vesi 2. Mutuwu ndi malangizo akuru a khalidwe lathu loyenera kwa Mulungu pa nkhani ya kulapa. Tikuona kuti kusala ndi mbali imodzi ya chivomerezochi. Tchimo lalikuru kudali kukwatira akazi a dzikolo.

10. Mutu 10 ukutseka bukuli ndi anthu akuvomeredza tchimo lao lokwatira akazi a mitundu, ndipo akuvomeredza kutsiya akaziwa achilendowa. Sitikudziwa vuto la akazi otsiyidwawo ndi ana.

Buku la Nehemiya likupitilidza nkhani ya kukhadzikika kwa Ayuda mu Yuda. Nehemiya ndi munthu amene amapemphera kwambiri chomwenso ndi chidzindikiro cha munthu wa Mulungu, palibe Kanthu kuti kodi izi zizatipangitsa kuti tilipire kutumikira Mulungu mokhulupirika. Nehemiya adali ndi udindo waukuru m'boma, ndipo adali nzake komanso wokondedwa ndi mfumu Aritasasta. Nehemiya adali okonzeka kutsiya udindo onona, ndikuika moyo wake pachiopsezo—inunso muli chimodzimodzi ndi mkuru ameneyu.

I. Nehemiya mutu 1 adalandira uthenga kuchokera ku Yuda zinthu sizili bwino. Panali patapita zaka 90 chipitire gulu loyamba lotsogozedwa ndi Zurubabelo ku Yerusalemu, koma kufikira nthawiyi zipupa zoteteza Yerusalemu zidali zitsanamangidwe. Kumbukirani kuti matsiku amenewo malinga/mpanda ndiomwe umazetsa chitetezo mu mzinda.

2. Mutu 1:4-11 tikunva kuyankha kwa umulungu kwa Nehemiya pa nkhani yonvetsa chisoniyi. Pali phunziro apa kwa ife. Tikuyenera kuphunzira pemphero lake ndikulitsunga, komanso kudziwa kuti kusala kudya ndi chinthu chabwino zedi.

3. Tsopano wazikonzekeretsa yekha, ndiokonzeka kuchita chinachake choopsa monga mutu 2 ukunenera adafunsa chilolezo kwa mfumu chopitira ku Yerusalemu. Ku Yerusalemu, adakayang'anira ntchito yomanga malinga ndipo monga ntsogoleri wabwino, adawaudza zakumanga malingawo kotero panalibe kubwerera m'mbuyo. Tikuona vesi 19 kuti adani ali tcheru mu dzina la Sanibalati ndi Tobiya.

4. Mutu 4 Nehemiya akulongotsola ntchitoyo, ndipo ntchito yomanga malinga tsopano ikupitilidzidwa. Mutuwu umanenanso za nsutso omwe unabwerapo ndipo Ayuda ena adapitilidza ntchito yomanga kachisimu, pamene ena adaima ngati alonda kuti alimbane ndi adani awo, ndikutetedza ogwira ntchitowa.

5. Mutu 5 tikuona kuyambirira kwa mtima wa Nehemiya, vesi 1-13 akunena kuti Nehemiya sadangokhala kapitawo chabe wa ntchito yamamangidweyo, komanso ndi ntsogoleri wa moyo wa uzimu. Muli njala yomwe ikupangitsa anthu kugulitsa malo awo komanso ena kuzigulitsa ku ukapolo kwa Ayuda olemera. Izi zikupangitsa Nehemiya kukhala okwiya, kotero adayankhula ndi olemerawo kuti asazuze abale awo osaukawo komanso kuwabwedzera katundu wao.

A. vesi 14-19 za kukana kwake kwa malipiro okwera ngati ntsogoleri wa dziko la Ayuda. Sadafune kuti akhale chipsinjo kwa anthu ake. Ichi ndichitsanzo cha ntsogoleri wabwino—timadzipereka nsembe kwa anthu athu.

6. Mutu 6 akunena za kulephera kwa anthu amene amafuna kutsokoneza ntchito yomanga kachisi. Vesi 15 akutiudza kuti malinga amalizidwa kumangidwa, ndipo izi zachitika modabwitsa kwambiri, chifukwa zangochitika kwa matsiku okwana 52 okha basi.

Ichi ndi chipambano chachikuru kwambiri chifukwa, tsopano mzinda wa Yerusalemu uli otetezeka kwa adani ake.

7. Mutu 8-10 ukuonetsa nthawi ya chisitsimutso cha uzimu mu Yerusalemu. Werengani 8:1-3 ndi 5-8 pamene tikuona anthu akutsonkhana ndi kuwerenga Mau a Mulungu. Dziwani izi kuti adaima tsiku lonse ndikunvetsera kuwerengadwa kwa Mau, padali a Levi (chitsanzo cha kulalikira) omwe amafotokodzera mauwa kwa anthu. Vesi 5 akutiudza za kukwezedwa kwa Ezara pamene amawerenga mauwa. Mofanana umo ndimomwe tiyenera kuchitira ndi M au a Mulungu. Tikuyenera kuchita nawo ndi ulemu wopambana, kuti tiwakweze. Zophunzitsa zathu zonse—zolalika zathu zonse zikuyenera kumangika pa Mau a Mulungu Baibulo.

A. Mutu 9:1-3 anthu amakumana pa nthawi ya kupembedza. Amatsala kudya ndi kulapa. Vesi 6-37 pali pemphero lalitali la anthu olapa machimo awo. Vesi 32-37 anthu

akudzindikira kuti Mulungu wachita mwa chilungamo ndi mokhulupirika ndi anthu ake. Akudzindikiranso kuti adachita mosakhulupirika ndipo adayenera chilango chomwe adachilandira. Adanena za kulapitsa kwa chilangocho.

B. Vesi 38 pa mutu 9 ndi Mutu 10:1-39 anthu akulemba ndi kusainira pangano la kulonjeza za kunvera kwa Malamulo onse a Mulungu. Ndondomeko za chisisimutsochi zidali, kusala kudya, kupemphera, ndi kulapa, kenako kufunsa Mulungu, kuti achotse chilango chawo chifukwa adalonjeza kunvera Mulungu. Ndikukhumba dziko lathu litachitanso chimodzimodzi.

Itapihta nthawi imeneyi, anthu adayambanso kupembedza mafano, komanso kukwatira akazi a chilendo ndipo adayamba kutsamala kwambiri lamulo m'malo mwa Mulungu mwini wake, ndipo munthawi ya Yesu tidali ndi Afalisi komanso a Saduki.

8. Mutu 12 akunena kuti anthu adapereka malinga awo atsopano ndi kulambira mu kachisi. Zinthu zili bwino ndi Ayuda.

9.mutu 13 ukunena za ulendo omwe Nehemiya adakonza kupita kwa mfumu, ndipo pamene adachoka mavuto adabweranso. Vesi 4-5 tikunva za Tobiya m'dani wa Ayuda, onani Nehemiya 2:10 ndi 4:7-8, adapatsidwa malo okhala mu kachisi. Uku kudali kupandukira Malamulo amene tikuwawerenga mu vesi 1. Ndipo pamene Nehemiya adabwerera ku Yerusalemu, adakonza vuto limeneli, onani vesi 6-9 pamene tikuwerenga kuti matabwa a Tobiya adatayidwa kunja kwa kachisi momwe Tobiyayu amakhala.

A. Timawerenganso mu chaputala 13 kuti anthu adalephera kusunga lonjezo lomwe adachita lonvera Mulungu. Nehemiya adagwiritsa ntchito nthawi yonseyi, kukonza anthu pamene adalephera kunvera Mulungu. Onani mu vesi 30-31 mau otsiridza a munthu weniweni wa Mulungu Nehemiya.

Nthawi zonse Mulungu ndi okhulupirika.

Estere

Estere ndi buku lopambana kwambiri mu Baibulo, ndilotsiyana ndi mabuku ena onse. Ndibuku lachiwiri mu chipangano Chakale lomwe linatchulidwa ndi zina la mkazi. Nkhaniyi idachitika moyambirira kupotsa buku la Nehemiya. Kudali ku Perisiya ku ukapolo pamene tikuwerenga za mtsikana amene Mulungu adamugwiritsa ntchito kuti apulumutse anthu ake ku chiwembu choopsa choononga anthuwa. Liwu loti Mulungu silikutchulidwa m'bukuli, koma tikuona kuti zanja la Mulungu likugwirira nkhondo ana Ayuda. Tikuona umboni m'buku limeneli la Estere pamene Mulungu asakulorela kuti anthu ake awonongedwe, ndipo mpingo wake sudzaonongedwa. Sindinena zambiri zokhudzana ndi Estere, monga nkhani yokoma ndi yotsangalatsa kuwerenga ndipo ndiyokhweka kuinvetsetsa.

1. Mbali yaikuru ya nkhaniyi ndipamene Ayuda adaopsezedwa kuti athedwa psiti. Ichi ndi chinthu chomwe chimachitaka mopitirira mu mbiri ya Ayuda. Akhristu ena amene adalakwitsidwa kwa nthawi yaitali akhala akuzunza Ayuda. Akatolika ndiolakwa pankhaniyi. Kumbukirani khoti la Chiroma lofufuza maganizo a anthu? Anthu a ku Germany adayetsetsa kupha Ayuda onse, munkhondo ya chiwiri ya padziko lonse.

Adapha pafupifupi Ayuda okwana 6 000 000. Lero, Asilamu amafuna atapha Ayuda onse. Koma Mulungu sadzalola adani kupanga zofuna zao koma adzawapanga iwo kukonda ndi kutetedza Ayuda.

2. Tikuona kuti tsoka la Ayuda limabwera motsogozedwa ndi ukulu wa Mulungu. ndizotsangalatsa kuti kachiwiri Mulungu wagwiritsa ntchito mzimayi kudalitsa anthu ake.

3. Imodzi mwa tchuti ya Ayuada yomwe amaichita mpaka pano, ndi tchuti cha Purim. Izi zimatanthaudza kuponya mayere kuti lidziwike tsiku lomwe ayuda onse adayenera kutheratu psiti. Ayuda pa phwando la Purim amatsangalala kuti Mulungu adapangitsa iwo kuti asaphedwa, koma m'malo mwake adali adani awo amene anaphedwa.

Nkhaniyi imatsekera Mbiri ya Chipangano Chakale. Mabuku ena onse amene tikhale tikuonawa adalembedwa mkati kati mwa nyengo ya mabuku omwe taona kalewa.

Buku la Estere lili ndi zigawo zinayi.

1. Ndondomeko ya chiwembu chomwe chimadikiriridwa 1:1-2:23. Mulungu adakonza zochitika zonse kuti Estere, mu Yuda adapangidwa kukhala mfumu kazi ndipo udindo umenewu patsogolo pake udathandidza kupulumutsa anthu a chiyuda.

2. ndondomeko ya choipa ikupangidwa 3:1-4:17 munthu woipa Hamani akukakamidza mfumu kuti alamulire kuti Ayuda onse aphedwe. Ziwani kuti pemphero ndi kutsala kudya zidali mkati mwa anthuwa.

3. pulani ya choipachi ikulaphereka onani mutu 5.

4. Anthu adapanga phwando chifukwa cha kupambanaku 9:18-10:3. Phwando la Purim limachitika kwa Ayuda mpaka lero chifukwa cha chipambanochi.

Yobu, Salmo, Miyambo, Mlaliki, Nyimbo ya Solomo

Tamalidza kuona mabuku omwe ndi ambiri, tsopano tikupitilidza ndi kuona mabuku amene amadziwika kuti ndi "olembedwa mwa ndakatulo." Awa ndi mabuku ovomeredzeka monga m'mene tiwoneremu. Nthawi zina mabukuwa amadziwika ndi dzina lakuti "Zolembedwa za mzeru" chifukwa umu muli malangizo a mzeru m'mabukuwa. Njira yabwino yophunzirira Masalmo ndi kuwerenga Salmo limodzi patsiku. Ine ndi mkazi wanga timawerenga pamodzi Salmo limodzi madzulo tisanapite kogona.

Yobu

Mipingo ya chipulotestanti inagawa Chipangano Chakale m'magulu anayi. Buku la Yobu ndi buku loyamba mu chigawo chomwe chimatchedwa mabuku a ndakatulo. Gawo ili la Baibulo lili ndi mabuku ngati Yobu, Masalmo, Miyambo, Mlaliki ndi Nyimbo ya Solomo. Yobu adakhalako nthawi ya Abrahamu kapena ntsogolo mwake. Ili ndi buku labwino kuliphunzira pamene uli m'mavuto. Lizakuthandidza kudziwa kuti

mavuto amafikira kwa munthu wina aliyense, ndipo kukhala nkhristu sikuti mavuto athera pomwepo. Tikudziwa bwino kuchokera m'Baibulo kuti, ambiri mwa anthu a Mulungu adakumana ndi mavuto. Ganizirani Yosefe, Mfumu Davide, Yeremiya ndi Paulo kungotchulapo ochepa chabe. Yesu Khristu nayenso adazunzika.

Buku la Yobu limaonetsa poyera kuti maulaliki olonjedza zinthu zabwino za kuthupi ndiolakwika. Mulungu sapereka chuma kwa akapolo okhulupirika chifukwa ndi okhulupirika ayi. Tikuwerenga m'buku limeneri kuti Yobu adataya katundu wake yense, komanso adazunzika koopsa ndi thupi lake. Koma Yobu akutiudza pa 1:1 kuti adali munthu wa Mulungu komanso kuti amaopa Mulungu ndipo analibe chilema. Izi zikutiphunzitsa kuti

1. Anthu a Mulungu amazunzikanso mu muthupi ndi m'maganizo. Mulungu nthawi zina amalamulira nsautso kwa anthu ake popanda chifukwa china chilichonse.
2. Anthu osalakwa amazunzikanso. Nkhristu nthawi zina amazunzika ngakhale kuti sadachite Kanthu koyenera kuti azunzike. Nthawi zambiri mazunzo a munthu amayamba ndi zinthu zomwe sitingazilongotsole. Onani Luka 13:1-5.

A. Nthawi zina munthu amavutika chifukwa cha tchimo lodziwika. Chitsanzo ndichakuti; kuchita chigololo ndi munthu wa kachilombo ka Edzi, zitha kupangitsa munthuyo kutenga matendawa ndi kumwalira nawo.

B. komabe nthawi zambiri, munthu amavutika, koma choyambitsa cha mavuto akewo sichingalodze ku tchimo lina lake.

3. Anthu a Mulungu amavutika koma kupitililabe kutamanda Mulungu. sakonda Mulungu nyengo za kukolola zokha ayi. Satana adayankhula pa Yobu 1:10-11 kuti Yobu akukonda Mulungu chifukwa zinthu zake zinali bwino. Yobu akuchitira umboni kuti munthu weniweni wa Mulungu, amakonda Mulungu ngakhale mu nthawi ya nsautso.

Ndondomeko ya Buku la Yobu

I. kulongotsola zokhudzana ndi Yobu (1:1-5)

1. Yobu amakhala kudziko la Uzi lomwe lili ku m'mawa kwa dziko la Israyeli. (1:1)
2. Yobu anadalitsidwa m'banja ndi chuma (1:2-4)
3. Yobu ndimunthu weniweni wa Mulungu (1:1 ndi 5)

II. Bwalo la kumwamba (1:6-12)

1. Mudali nsokhano m'mwamba wa angelo (ana a Mulungu). pankumanowu padali Satana amene amaneneza Mulungu ngati Yobu ali wolungama kapena ayi
2. Mulungu akumuudza Satana kuti Yobu ndi munthu wolungamadi. (1:8)
3. Satana adayankhula kuti chinthu chomwe chikupangitsa Yobu kukhala olungama ndi chifukwa cha madalitso a Mulungu. (1:9-11)
4. Mulungu adalola Satana kumuyetsa Yobu potenga china chilichonse cha Yobu, kungopatulapo moyo wake, dziwani kuti Satana atha kungochita zokhazo zomwe walamulidwa ndi Mulungu. (1:12)

III. Nyengo ya Msautso (1:13-22)

1. Amithenga anayi anabweretsa uthenga wa kuonongeka kwa chuma chake ndi ana ake. Mauthengawu amabwera mofulumira ndi motsatizana, ndipo kanthawi kochepa Yobu adachoka pa munthu wa Chuma ndikukhala mphawi, komanso kuchoka pa utate kukhala opanda mwana. (1:13-20).

2. Yobu adadzichepetsa ndikuzindikira kuti Mulungu ndi amene amalamulira pamene tili kapena tilibe Chuma; tinabwera m'dziko opanda Kanthu ndipo opanda kanthunso tidzapita. Izi zikutiosa ife kutsiya pachuma chathu kufunikira kochepa. (1:21)

3. Yobu sadazuzule Mulungu kuti adachita china chilichonse cholakwika. Yobu adavomeredza kutayika kwa katundu wake, koma pazonsezi Yobu sadalakwire Mulungu. (1:22)

IV. Bwalo la kumwamba kachiwiri (2:1-6)

1. Mulungu ndi Satana akukumana kachiwiri. Mulungu akunyada pamaso pa Satana kuti Yobu sadataye Mulungu chifukwa cha mavuto ake otsasimbika. (2:1-3)

2. Satana adati izi zikuchitika chifukwa thupi la Yobu silinakhudzidwe, koma katundu wake yekha, ndipo kuti Yobu azanyoza Mulungu thupi lake likakhala kuti laonongedwa. (2:4-5)

3. Mulungu kachiwiri akuonetsa kuti akulamulira zinthu zonse ndipo akulorera Satana kukhudza thupi la Yobu; koma asatenge moyo wake, (2:6).

V. Nyengo ya nsautso ikudzanso kawiri (2:7-10)

1. Kusauka kwa Yobu nthupi lake motsowetsa ntendere. (2:7-8)

2. Mkazi wa Yobua kupereka malangizo olakwika pakuudza mwamuna wake kuti atukwane Mulungu. (2:9)

3. kupatula chili hconse chidachitika kwa iye, Yobu adakhalabe okhulupirika kwa Mulungu. (2:10)

4. Yobu sakudziwa chifukwa cha kutsauka kwake. Sakudziwa kuti Mulungu akumuyang'ana ndi diso la chifundo ndi chiyamiko. Mulungu mwachiyembekezo adalotsera zotsatira za matsautso ake.

VI. kufika kwa Anzake a Yobu (2:11-13)

1. Anali okhudzika kuona kuzunzika kwakukulu komwe Yobu amadutsamo, kufikira kuti samatha kumuzindikira mzawoyo, ndipo adasowa choyankhula kwa sabata ya nthunthu. Yobu 7:5 akutipatsa chitsanzo cha maonekedwe oyipa a Yobu.

VII. Yobu alephera kupirira (3:1-26)

1. Yobu anautsanza mtima nayamba kuyankhula modamdaula. Adafunsa chifukwa chimene anabadwira ndipo adafunafuna imfa.

VIII. Anzake a Yobu atatu Elifazi, Bilidadi ndi Zofa ayankhulapo (4:1-31:40)

1. Anzake a Yobuwa amayankhula motsogozana ndipo pakuyankhula kwa aliyense Yobu amayankhapo. Anzake a Yobu sadamutonthodze iye. Aliyense motsalondola adanena kuti kuzunzika kwa Yobu kunadza chifukwa cha tchimo. Adayankhula kuti kuzunzika kwa Yobu kunabwera chifukwa Yobu ndi ochimwiratu.

IX. Elihu nzake wina wa Yobu akulowanso mu zokambiranazi (32:1-37:24)

1. ndiokwiya ndi Yobu akuzilungamitsa yekha m'malo molungamitsidwa ndi Mulungu. (32:2)

2. ndiokwiya ndi anzake ena a Yobu chifukwa adati Yobu ndiolakwa koma adalibe yankho labwino. Tisamanene chilichonse pomwe sipanthawi yake. (32:3)

3. Elihu anathirapo ndemanga kuti mazunzo ena amadza ngati chizuzulo, ndipo chomwe chili choyipira thupi chimakhala chokomera mzimu.

X. Mulungu akuyankhulapo (38:41-44)

Motsindika Mulungu adanenetsa kuti Yobu ndi anthu onse sadzindikira zochitika za dzikoli. Sitimanvetsetsa momwe zolengedwa zimagwirira ntchito, choncho, sitingayembekedzera kunvetsetsa m'mene Mulungu amachitira ndi zolengedwa zake. Ife anthu tili ndi malire pa mphanvu zathu zakuchita polamulira zinthu zochitika, tili ndi nzeru za malire posanvetsetsa m'mene zinthu zikuchitikira.

1. Mulungu pa mutu 38-39 akumuudza Yobu kuti Iye yekha ndiyemwe ali ndi mphamvu yolamulira zochitika zili zonse, ndipo Mulungu m'mene analengera zonse komanso m'mene adapangira Malamulo omwe zolengedwa mu kagwiridwe kake ka ntchito zingamachitire. Yesaya 45:7 akutiphunzitsa kuti ndi Mulungu amene amapangisa zovuta zonse angakhale nthenda ya misala.

XI. Yobu ayankha Mulungu (42:1-6)

Yobu akuchepetsedwa ndi Mulungu ndikuvomeredza kuti walakwitsa. Ndipo akuvomeredza kuti Mulungu ndi wa nzeru zonse, ndipo pamene sadziwa chifukwa cha kudza kwa masautso ake, Yobu akudzindikira kuti mfunso la "chifukwa ninji" silofunikira. Yobu akuzindikira kuti Mulungu ali pampando wachifumu ndipo akuchita chomwe chili chabwino kwa iye. M,mawu ena Yobu adakhulupirira Mulungu kotheratu ndipo adalapa chifukwa amafunsa Mulungu mafunso.

XII. Yobu akubwedzeretsedwa mu ulemerero wake ndi Mulungu (42:7-17)

Mulungu anadzuzula Elifazi, Bildadi ndi Zofa. Mulungu sadangobwedzeretsa chuma chomwe m'mbuyomo Yobu adali nacho koma anachichulukitsa kawiri ndi chuma adalinacho.

1. Banja la Yobu linabwera ndikumutonthodza chifukwa cha chipsinjo chimene Mulungu adamuikira. (42:11)

Khristu ndi mpingo wake

I. chinsinsi cha masautso kapena chakuti ndichifukwa ninji kuli matsautso.

1. mavuto alipo chifukwa cha tchimo padziko lapansi. Kotero wina aliyense kuphatikidzapo nyama amakumana ndi mavuto chifukwa cha tchimo la dziko lapansi.

2. zifukwa zina zomwe anthu amavutikira.

A. Nthawi zina munthu amavutika chifukwa cha zitsankho zolakwika kapena kutsatsamala kwa munthuyo.

i. chitsanzo ndi chakuti pamene munthu wasankha kusuta fodya, ndikuyamba nthenda ya kansala ya mu mapapu ndikuzunzika nayo mpaka kufa.

B. Nthawi zambiri timazunzika koma otsadziwa chifukwa chomwe tikuvutikira

i. Anzache a Yobu adamuudza kuti akuzunzika chifukwa cha tchimo lake. (Yobu 4:7-8 ndi Yobu 8:4). Timadziwa kuti ichi chinali chifukwa cholakwika kwambiri. Yobu 1:8 akutiudza kuti Yobu adali munthu wolungama ndi wangwiro, ndipo kuvutika kwake sikunadze chifukwa cha choipa chomwe Yobu anachita.

ii. Musakhale ngati anzake a Yobu, amene nthawi zambiri, amamuudza Yobu kuti tchimo lake ndilimene lapangitsa kuti akumane ndi masautso. Yobu (8:4-6; 5:17;11:14) nthawi zambiri sindingadziwe mwatsatanetsatane chifukwa chimene chikupangitsa munthu kumti azivutika. Ganidzirani zimene Yesu adanena pa Yohane 9:1-3 kuti mutsimikidzire kuti kuzunzika kwa munthu kutha kusakhudzana ndi tchimo lake.

a. ngakhale titakhala kuti sitinazindikire tchimo lomwe lapangitsa munthu kuti avutike titsayenjedzere kwa iye chifukwa chomwe chamupangitsa kuti avutike. Nzako weniweni azakutonthodza popewa nsutso. Ingoperekani chitonthozo osati kuweruza ayi.

b. Yobu 19:13-19 akutiudza momwe banja lake la Yobu lidamukanira ndikuyenjedzera ululu ku mavuto ake.

3. Elihu adapereka yankho loyenera lomwe limaonetsa chifukwa chomwe nthawi zina timavutika, pamene adati ndinjira ya Mulungu kuphunzitsa, kuzuzula, ndi kukonza Yobu, ngakhale ichi chidali chifukwa cholakwika pa nkhaniyi.

A. Ahebri 12:5-11 akutiphunzitsa kuti chidzuzdzulo ndi chidzindikiro cha chikondi cha Mulungu pa ife.

i. Yankho la ngwiro la Mulungu, ndilakuti mavuto ndi yetsero lakukhulupirira Mulungu molingana ndi momwe iye alili, otsati zomwe iye amachita.

4. Yesu akutsimikidzira kuti munthu atha kukhala wolungama kwanthunthu komabe kukumana ndi mavuto. Yesu adali otsachimwa koma adazunzika kupotsa munthu wina aliyense angakhale kufika pamulingo wa kuikidwa pantanda. Adanva mavuto a mthupi pakupachikidwa pantanda ndipo adazunzikanso pamene adalekana ndi Mulungu Atate mwa kanthawi.

5. Yobu akunena monveka bwino ulosi okhudzana ndi kuuka kwa Khristu ndi mpingo wake. (Yobu 19:25-27) iyi ndi nfundo yomwe ikuonetsa chikhulupiriro cha Yobu mwa Mulungu, ngakhale Yobu akuvutika kotsalekedza.

Zoti tiphunzirepo

1. Mulungu ndiyemwe akulamulira. Palibe chingachitike pokhapokha ngati wachilola kuti chichitike. (Danieli 4:34-35; Masalmo 115:3)

2. Mdani wankhuru Satana ndiwamphanvu kwambiri (1Petro5:8). Koma mphamvu zake pamaso pa Mulungu zili ndi malire. (Yobu 1:18 ndi Yobu 2:6)

A. Tisamanyodzetse mphamvu ya Satana. Ndiwamphamvu kuti sitingathe kulimbana naye pogwiritsa ntchito mphamvu zathu. (Yuda 1:9) Tipemphe Mulungu kuti atitetedze ku zotiphinja zake.

B. Yesu yekha adalimba kulimbana ndi mayetsero a Satana mpaka adawagonjetsa. Adamugonjetsa Satana pamene adapachikidwa pa mtanda.

3. Kupenya chifuniro cha Mulungu.

A. Abwenzi a Yobu adagwuritsa ntchito njira yachabe poonetsa chifuniro cha Mulungu. Elifazi adagwiritsa ntchito maloto ndi maso mphenya. (Yobu 4:12-16) Bildadi adagwiritsa ntchito zachikhalidwe chomwe chidapita mu m’badwo wam’mbuyomo (Yobu 8:8-10). Zofa adagwiritsa ntchito kaonedwe ka zinthu ndi kaganidzidwe (Yobu 20:2-3).

B. zaka 4000 patsogolo pake, Baibulo litamalidzidwa kulembedwa, anthu akuyetserabe kutsogolera anthu njira yotaika pogwiritsa ntchito maloto, maso mphenya, zikhalidwe za makolo, kaonedwe ka zinthu (experience) ndi kaganizidwe.

C. tikuyenera kunvetsetsa kuti Mulungu sayankhula nafe kudzera mu maloto, kapena mu maso mphenya chifukwa Baibulo tsopano ndilokwanira (Chivumbulutso 22:18). Zachikhalidwe cha makolo monga ufiti zukutisocheretsa zedi. Anthu m’makono

akugwiritsa ntchito kaonedwe ka zinthu ndi kaganidzidwe zomwe akumazitchula sayansi (science), ndikutsokeretsa nawo anthu.

D. Njira yabwino yoonera chifuniro cha Mulungu, ndikutsatira ziphunzitso za m'Baibulo ndi kupemphera.

4. zinthu zonse zimathandidzana kuchitira ubwino, ngakhale m'mavuto athu (Aroma 8:28). Akhristu akuyenera kukumbukira kuti mavuto omwe tikukumana nawo lero safanana ndi ulemerero omwe ukudzawo (Aefeso 1:3; 2Akolinto 4:17)

A. Akhristu tikuyenera kuzindikira kuti pokhala moyo uno tikuyenera kukonzekera moyo osatha. Kuzunzika kwathu ndi kwa nthawi yochepa, pamene kumwamba kukakhala kwa muyaya.

Mathero

1. Phunziro lalikuru kuchokera mbuku la Yobu ndilakuti Mulungu nthawi zonse amadziwa zomwe akuchita ndi zifukwa zomwe akuchitira zimenezo. Tiyende ndi chikhulupiriro otsati ndi maso a kuthupi. Tikuyenera kukhulupirira kuti Mulungu nthawi zonse amadziwa chomwe chili chotiyenera potsayang'anira nyengo yomwe tikudutsamo. Tikuyenera kukumbukira kuti Mulungu ndi amene amalamulira zonse.

2. kunzunzika ndi mbali imodzi ya moyo ndipo izi sizizachoka kwa ife. Chipangano Chatsopano, chimatiphunzitsa kuti Mulungu ali ndi zifukwa zotipangitsa ife kuti tizunzike.

3. Mulungu safuna kuti tiyankhule chilichonse pazomwe azilola kuti zichitike.

Masalmo

"Makalata a chikondi a Mulungu kupita ku Mpingo"

Bukuli lili ndi olemba ambiri kuphatikidzapo Davide amene adalemba theka la Masalmowa. Masalmowa ali ndi chilakolako cha anthu kuchokera pansi pa chisoni kupita mathero a chimwemwe. Masalmo agwiritsidwa kwambiri ntchito mu Chipangano Chatsopano pafupifupi maulendo 116.

Masalmo ambiri akunena za momwe tingapembedzere Mulungu moyenera.

Muli masalmo a mitundi yokwana khumi;

1. Ophunzitsa=Masalmo omwe akupereka ziphunzitso monga 1,4,7,15, 17, 50, 73, 94, 101.
2. Mbiri=78, 105, 106, 136.
3. Olemekedza Mulungu/Haleluya=106, 111, 113, 115, 117, 135, 146-50.
4. Kulapa ndikuvomeredza machimo=6, 32, 38, 51, 102, 130, 143.
5. Mapembedzero= 86.
6. Kuthokodza= 16, 18.
7. Mesiya= 2, 20-24, 41, 68, 118.
8. Chilengedwe= 8, 19, 28, 33, 65, 104.
9. Ulendo opita kunyumba ya Mulungu monga ulendo opita ku Yerusalemu=132-140.
10. Matemberero=35, 52, 58, 59, 83, 109, 137, 140.

Tione zina mwa zochepa zitsanzo;

1. Chiphunzitso werengani Salmo 15. Vesi 1 ikufunsa amene akulandiridwa ndi Mulungu. Vesi 2-5 akutiudza makhalidwe oyenera, makamaka vesi 2.
2. Masalmo a Haleluya, werengani 113 malangizo okoma polemekedza Mulungu.
3. Zokhudzana ndi kulapa werengani 32:1-4 tikuphunzira kuti okhululukidwa okha ndiomwe ali ndi chimwemwe chenicheni. Vesi 5-11 tikuphunzira za kulapa ndipo vesi 11 akunena zokhudzana ndi chimwemwe chenicheni.
4. Masalmo 86 akutiphunzitsa m'mene tingapemphere kwa Mulungu moyenera.
5. Masalmo 16 akutiphunzitsa momwe tingathokodzere Mulungu.
6. Nthawi zina Salmo limayamba kuyankhula ngati likunena za mfumu ya kudziko, koma izi zimakwaniritsidwa kwanthunthu mwa Yesu monga Maslmo 2. Ena mwa iwo amanena za mfumu Davide, koma ena monga vesi 7 atha kukhala kuti akutanthaudza za Yesu. Salmo 22 ndi Salmo yomwenso ikunena za Mesiya, ndi Salmo ya ulosi wonena za Yesu ntsogolomo. Onani Salmoli kuti muone kulongotsola konveka bwino za Yesu, pamene adzapachikidwe. Onani vesi 1 kuti muone mau amene Yesu adanena zaka zambiri zapitazo kenako pamtanda onani Mateyu.
7. Salmo 109 limadziwika kuti Salmo la matemberero. Izi zimatizunza pamene zikunena za matemberero pa wina wake monga m'mene msing'anga amachitira. Werengani vesi 6-11 kuti muone momwe wina akupemphera Mulungu kuti achotse mdani wake. Akhristu a mbiri amavutika m'maganizo chifukwa cha nkhanza za Salmo limeneli. Dziwani izi kuti mavesi amenewa amaitana Mulungu kuti athane ndi olimbana nawe; osati iwe kuchita chiweruzo pa anthuwo ayi. Ine njira yanga yomwe ndingatsate zitandichitikira izi ndikungopempherera munthuyo kuti alape ndi kubwera kwa Yesu ndikuti Ambuye alowe m'malo mwa munthuyo.
8. Tiyeni tione Salmo lalikuru lachitonthozo mu nthawi ya mavuto. Salmoli lidali lotchuka ku America masiku a m'mbuyomu Baibulo likuloledwa kuti liziwerengedwa m'masukulu. Ophunzira ambiri adali ndi chizolowezi chocholoweza Salmoli. Patha zaka 40 tsopano kuchokera pamene kudalamulidwa kuti kuwerenga Baibulo ku Sukulu ndi kuphwanya Malamulo, ndipo zaka 40 za kupanda khalidwe zatsatira pambuyo pake. Tiyeni tiwelenga Salmo 23.

Miyambi

Miyambo yambiri idalembedwa ndi mfumu Solomo, inanso idalembedwa ndi Hezekiya pamene yochepa idalembedwa ndi anthu ena. Tanthaudzo la buku la Miyambo ndi lokopa moyo lomwe litanthaudza kuti kuphunzitsa choonadi. Miyambiyo ikunena za chilichonse cha padziko lapansi. Miyamboyi ndi malangizo abwino, koma si malonjezo ayi. Cholinga chawo ndikulimbikitsa ife kukhala m'moyo wolungama pamatso pa Mulungu. ambiri ndi osavuta kuwanvetsetsa, koma alipo ena omwe ndiovuta kuwanvetsetsa.

Miyambo ndiyabwino kwa anthu a nsikhu uli wonse, ndipo ina ndi yabwino mwa paderadera kwa achinyamata monga 1:8-10, 3:11, 5:20, 10:5 ndi ina yotere. Ili ndi upangiri wa momwe anthu a chichepere angachitire, kuti akhale ndi moyo, ndikupewa mavuto ambiri akudza m'moyo uno. Maphunziro akuru a Miyambo ndi tchimo, kukhulupirika, anthu oipa, maubale; makamaka zinthu zonse zomwe timakumana nazo m'moyo uno.

Zolinga zisanu za Miyambo ndi

1. Kupedza nzeru ndi mwambo onani Miyambo 1:2. Baibulo limatiudza kuti nzeru ndi mwambo zimachokera kwa Mulungu onani Yobu 28:12-18, 21 ndi 23.

2. Miyambo 1:2 akuti miyamboyi imatithandidza kunvetsetsa mau owona. Adzatithandidza kunena choonadi m'malo mwa maboza monga pamene anthu akufuna kuti atiputsitse. Mwachitsanzo adzatithandidza kuunikira nfundo zoti tiyankhule ngati china chke chili bwino ndi ife. Chitsanzo ndichakuti sitimakhulupirira zomwe munthu akunena zokhudzana ndi Baibulo pokhapokha titaona ngati Baibulo likunenadi zimenezo. Aphunzitsi ambiri onama adzakuudzani kuti Mulungu akulonjeza kuti akhristu azakhala achuma kapena amati "Mulungu amathandidza odzithandidza okha." Monga mukuphunzira kuonetsa choonadi kapena kunena choonadi, tikuphunzira kuyang'ana m'Baibulo pa ife tokha tisanaganidze kuti cholondola ndichiti.

A. Ahebri 5:14 akutiudza kuti akhristu okhwima ali ndikuthekera kopotsa kunena choonadi kutsiyana ndi bodza. Ndikwabwino kunvera akuru, komabe mukuyenera kuonetsetsa kuti zikunena akuluzo ndi zoona.

3. Miyambo 1:3 akunena kuti Miyambo zoti tiphunzire m'mene tingakhalire olemekedzeka ndikuchita chomwe chili chabwino ndi chokoma. Amatithandidza ife kukhala m'njira yomwe ingatsangalatse Mulungu. Timaphunzira pa Miyambo 11:1 kuti Mulungu amafuna ife kuti tikhale okhulupirika m'mabizinezi athu ndikuti tisanamidze wina aliyense.

4. Miy. 1:4-5akutiudza kuti Miyambo imatiphunzitsa kuti tiyenjedzere nzeru zomwe tili nazo. Vesi 4 ikuti Miyambo imaphunzitsa achichepere, koma vesi 5 ikunenanso kuti Miyambo imalangidza kuti wanzeru amve nayenjedzere nzeru komanso kuphunzitsa akulu. Tikonzeke kuphunzira potsawerengera kuti ndi ife akuru bwanji. Palibe anganene kuti ine ndiwankuru kwambiri kotero sikoyenera kuti ndiziphunzirabe. Munthuwa wanzeru amadziwa izi, koma wopusa amaganidzira kuti akudziwa zonse kale, kotero safuna kuphunzitsidwanso.

5. Miy. 1:6 tikunva kuti Bukuli limatiphunzitsa kuganidza ndi kufufuza mokuya zinthu zomwe zili zofunikira kwambiri, monga ngati choona chochokera m'Baibulo. Anthu ambiri amawerenga mavesi a Baibulo mothamanga, kotero amangoona choona cha pamwambamwa. Pali zambiri zomwe tingaphunzire m'Baibulo, zomwe tingaziphunzire pamene tiwerenga Baibulo mofatsira, kawirikawiri, pamodzi ndi pemphero. Mwachitsanzo, tanthaudzo lapamwambamwamba la Yohane 3:16 ndilokhweka kuti aliyense atha kunvetsetsa koma pamene tiphunzira vesi limeneli kawirikawiri tidzakhala tikuphunzira za chikondi chopotsa cha Mulungu nthawi zonse pamene tiwerenga vesiyi.

Miyambo imatiphunzitsa zinthu m'madera otsiyanatsiyana monga;

1. Kukwiya Miy. 14:17, 29, 15:18; 16:32; 19:11 mavesiwa akunena momwe tingapewere kukwiya. Anthu ambiri amapsa mtima zotsatira zake amatha kuvulaza anzawo kapena kupha kumene, chifukwa alephera kugwira nkwiyo wao.

2. Chifundo, Miy. 3:9-10; 11:24-26; 14:21, 19:17; 22:9 akutiphunzitsa kuchita chifundo. Akhristu amadziwika pochita ntchito za chifundo.

3. Mwambo-Miy. 13:24; 17:6; 19:18; 22:6,15; 23:13-14 akutiphunzitsa zokhudzana ndi ana, ndi mmene mwambo/chidzudzulo kwa ana kuphatikidzapo kumenya ndizabwino kwa ana. Timachita izi chifukwa timawakonda anawo. Miyambo 3:11-12 tikuphunzira kuti, ngati ife tili mwa Mulungu, adzatidzudzula chifukwa amatikonda, onani Ahebre 12:5-11 kuti muone zambiri za ganizoli.

4. Kuopa Mulungu—Miy. 1:7; 3:7; 9:10; 10:27; 14:26-27; 15:16,33; 16:6 19:23; 23:17; 24:21 onsewa akunena za kuopa Yehova. Tichitire Mulungu ulemu ndi

kumulemekedza Iye, ndikudziwa kuti ndioopsa. Osakhulupirira salabadira za mphamvu ndi chiweruzo choopsa cha Mulungu.

5. Zisiru—Miy. 10:18,21,23, 12:15-16; 14:9; 15:2, 17:10, 12,24 20:3; 23:9; 27:22; 28:26 akutiphunzitsa za zisiru.

6. Abwenzi—Miy. 17:17; 18:24; 19:4; 27:10 akutiphunzitsa zokhudzana ndi abwenzi

7. Kugwira ntchito—Miy. 6:6-11; 10:4-5, 12:27; 13:4; 15:19; 18:9, 19:15,24; 20:4,13; 24:30-34; 26:13-16 akutiphunzitsa kuti tisakhale aulesi koma ogwira ntchito molimbika.

8. Momwe tingachitire ena—Miy. 14:31; 22:22; 28:16 akutiphunzitsa kuti tisaponderedze anthu; koma kuchita ndi aliyense mwa chifundo ndi mwa chilungamo.

9. Kunyada—Miy. 6:17; 11:2; 13:10; 15:25;16:18-19; 18:12; 21:4,24; 29:23; 30:13 akutiphunzitsa zokhudzana ndi kuopsa kwa kuzitukumula/kunyada.

10. Kuchita ntendere—Miy. 3:30; 10:12; 15:18; 16:28; 17:1,14, 19; 18:6,19; 20:3; 22:10; 25:8; 30:33 akutiudza kuti tikhale osungitsa ntendere m'malo mobweretsa makangano.

11. Kugwiritsa ntchito lilime—Miy. 4:24; 10:11-14, 17-21, 31-32; 12:17-19,22; 13:3; 14:3; 15:1-2,4-5,7,23; 16:13, 23, 27; 17:4; 18:6-7, 21; 19:1akutiphunzitsa za kuopsa kwa lilime lotsadziretsa. Werengani Yakobo 3:1-10 kuti muone zambiri zokhudzana ndi lilime.

12. Chuma—Miy. 10:2,15; 11:4, 28; 13:7, 11; 15:6; 16:8; 18:11; 19:4; 27:24; 28:6,22 akutipatsa nzeru zochuluka zokhudzana ndi chuma komanso katundu.

13. Mkazi woipa—Miy. 2:16-19; 5:3-14, 20; 6:24-35; 7:5-27; 9:13-18; 23:27-28 akutiphunzitsa kukhala kutali ndi mkazi woipa ndi wachigololo.

13b. Mkazi—Miy. 5:18-19; 11:16; 18:22; 19:14; 31:10-31 akutiphunzitsa kuti mkazi woopa Mulungu ndi mphatso yopambana yochokera kwa Mulungu ndipo tidzakondwera nayo.

14. Nzeru—Miy. 1:7, 20-22; 2:6-7, 10-11; 3:13-18, 19, 21; 4:5-9; 8:1-16; 9:1-6;12:8; 14:8; 18:4; 19:8; 24:3 akutiphunzitsa ife kuti nzeru imachokera kwa Mulungu. Tingapedze nzeru zochuluka pamene tiphunzira Baibulo. Makolo ndi akuru oopa Mulungu angatiphunzitsenso ife nzeru zopotsa.

Buku la Miyambo ndi muuni wabwino kuti tikhale moyo weniweni wa chikhristu lomwe lilinso ndi malangizo enieni azinthu zochitika ndipo ndilofananako ndi buku la Chipangano Chatsopano la Yakobo. Muphunzire miyambo yonse ndikuwerenga chaputala chimodzi kapena theka la chaputala nthawi imodzi.

Mlaliki

Ilinso ndi buku lina la nzeru. Olemba wabukuli sadziwika kwenikweni, koma ambiri amati bukuli lidalembedwa ndi mfumu Solomo. Adakhala moyo wake mwa njira yoti bukuli likulongotsola m'mene amanvera maka pamapeto moyo. Tikuwerenga za munthu yemwe ananva chitsoni malinga ndi momwe anakhalira m'moyo wake.

Tikudziwa bwino kuti Solomo adayamba moyo wake ndi chiyembekedzo chachikuru; tikukumbukira kuti Mulungu adamupatsa nzeru zochuluka ndi chuma chopambana. Solomo sadakhutitsidwe ndipo hadafunafuna chuma chochuluka kupotsa apa, komanso adayamba kupembedza mafano. Tsopano pamapeto pa moyo wake, adazindikira kuti moyo opanda Mulungu patsogolo pa zonse ndi moyo opanda kanthu.

Zinthu zopambana zomwe ndi ndizotsatha ndizomwe tichitira Mulungu. Solomo ndiwachisoni pamapeto pake chifukwa wakhala akuseweretsa moyo wake ndi zinthu zopanda pake za moyo uno mmalo mopereka moyo wake kutumikira Mulungu ndikupembedza Iye.

Ili ndi phunziro lomwe anthu ambiri salipedza kufikira moyo wawo utangotsala pang'ono kuchoka pano padziko. Zinthu zomwe timadzitsiya kumbuyo, ndizopanda pake monga nyumba, udindo wathu monga kukhala ngati mfumu, kapena munthu olemera kwambiri. Tidzapita ndichani pochoka padziko lino? 2Timoteo 4:8akunena za korona wachilungamo yemwe Yesu adzapereke ngati mphoto kwa ife, pamene tikulowa kumwamba, chifukwa tikuudza anthu zokhudzana ndi Iye. Tidzakahla m'chiyanjano ndi anthu amene adzapite kumeneko chifukwa tidawaudza za pulani ya Mulungu yokhudzana ndi chipulumutso. Tiyeni tione mwachidule zomwe zili mbukuli.

I. Tikuonamo moyo womwe uli ndi magawo awiri. Woyamba tikuona anthu omwe akukhala monga mwa thupi, monga amachitira munthu osaopa Mulungu. Mbali ina tikuona munthu yemwe akudziwa Mulungu. Cholinga cha Mlaliki ndi kuonetsa anthu soka lakudza chifukwa cha kutsata zinthu za kuthupi ngati cholinga chenicheni cha moyo wao, ndikulodza kwa Mulungu ngati nkhokwe ya chinachilichonse cha bwino.

1. Kalikonse kochita munthu ndi kopanda ntchito ngati alibe Mulungu. Ndiphindu kukhala mm'moyo womwe Mulungu ali patsogolo pa zonse.

2. ndi ntchito ya Mulungu yokha yomwe imakhalabe mpaka matsiriziro, kotero ndi Iye yekha amene angapereke kufunikira ku moyo wa munthu ndi kutumikira kwake.

II. Zachabechabe

1. Zinthu khumi zachabechabe

Mzeru za munthu 2:15-16

Ntchito za munthu 2:19-21

Zolinga za munthu 2:26

Udani wa munthu 4:4

Moyo wa munthu okhumba chuma 4:8

Kutchuka kwa munthu 4:16

Kutsakhutisidwa kwa munthu 5:10

Kukhumba kwa mtima 6:9

Madyerero m'malo mokhadzika olira 8:10, 14

Bukuli likumalidza pa mutu 12:9-14 ndi ganizo lakuti anthu onse amadalira pa Mulungu. vesi 13 ndi kiyi wa mutu 12. Mathero a zokamba akuti zonse zamveka. Opa Mulungu ndikusunga Malamulo ake, pakuti iyi ndiye ntchito yaikuru yomwe munthu ayenera kuchita. Mauwa muchiyankhulo chenicheni adalemba kuti "pakuti ichi ndicho cha mtundu wa anthu." Kumvera Iye ndiko kukhala munthu weniweni ndikufikira mulingo wopambana monga mbali ya chilengedwe. M'mawu ena, kupambana kwathu kumapedzeka pamene tili mu ubale wathu ndi Mulungu.

Nyimbo ya Solomo

Iyi ndi Nyimbo ya chikondi, ndipo vesi 1 ikuti nyimboyi idali ya Solomo. Ena amaona ngati iyi ndi Nyimbo yonena za chikondi cha Mulungu ndi anthu ake a Israyeli. Anthu ena ngati ine timaganidzira kuti nyimboyi ndi chikondwerero cha chikondi pakati pa abwenzi achichepere omwe adalengedwa mu chifaniziro cha Mulungu. Kuika buku ngati ili

m’Baibulo, zikungoonetsa poyera kuti Mulungu amasangalala ndi zimene munthu amachita. Ubale wapakati pa mwamuna ndi mkazi wake ndiofunikira pambuyo pa ubale wina ofunikira kwambiri ndi Mulungu. Taonani kufunikira kopotsa kwa ubalewu! Banja labwino limapereka ulemu kwa Mulungu, ndipo ndi malo a bwino olerera ana a mbadwo wa m’mawa kuti akhale anthu a Mulungu.

Mafotokozedwe ena m’bukuli ndi a chilendo kwa ife monga mutu 4:1-5. Iyi idali njira yoyenera yoonetsa chikondi chako kwa kabuthu mu m’badwo wa matsiku amenewo. Anthu ambiri samanva bwino ndi mau okhudzana ndi kugonana omwe ali m’bukuli. Mulungu amalongotsola monveka bwino kuti kugonana mu chikondi cha pakati pa anthu omwe ali m’banja mwamuna ndi mkazi ndi chinthu chabwino kwambiri.

Phunziro la Baibulo: Anthu m’madera athu akutsocheretsedwa pa nkhani ya kugonana, zomwe nthawi zambiri zimathera mmavuto kwa iwo amene amachita nchitidwe ogonana motsayenera. Bukuli likutidzindikiritsa kuti ziwalo zomwe zimagwiritsidwa ntchito pogonana ndi mbali imodzi ya chilengedwe chopatulika cha munthu. Mulungu adalenga ife “mwamuna ndi mkazi” ndipo ambiri mwa ife ndiotsangalala kuti Mulungu adatilenga choncho. Kulumikidzana kwa muukwati kumamanga ubale wa anthu (Genesis 2:24), ndipo palibe amachita manyazi (Genesis 2:25). Bukuli limachitira umboni kuti amuna ndi akazi amathandizirana wina ndi mzake pamene akhala mu ubale wa ukwati pakati pa mwamuna ndi mkazi. Zimatsimikidzira kuyeretsetsa kwa banja ndikutsimikidzira kugonana, kwa anthu omwe ali muchikondi pakati pa mwamuna ndi mkazi mkati mwa banja. Dziwani kuti umathanyula (kugonana pakati pa anthu ofana ziwalo) ndi kugonana kunja kwa banja siziloledwa mpaka kalekale.

Kuona za Aneneri

Gawo lalikuru ndi lotsiridza mu Chipangano Chatsopano ndi la aneneri. Kasanjidwe ka mabukuwa sikali kolingana ndi nthawi yomwe adakhalako zomwe zikutanthaudza kuti, mabukuwa sadasanjidwe mundondoko molingana ndi momwe zinthu zinachitikira. Utumiki wa aneneriwu ndi umboni kuti Mulungu amatikonda. Munthu atasankha kuchimwa, adali pa nkhondo ndi Mulungu, ndipo adaweruzidwa kuti apite ku Gahena. Koma mofulumira Mulungu adayamba kuchita ntchito yoombola munthu. munthu adalibe kuthekera kochita zinthu zabwino pa iye yekha, kotero Mulungu adatumidza aneneri kuti athandidzire anthu kuti abwerere kwa Iye kuchoka ku uchimo wawo. Komabe kuyetseraku kudalephera, koma chiyembekedzo chiyembekedzo chimodzi chokha cha ntundu wa anthu ndi Mpulumutsi wathu—Yesu Khristu.

Chomwe mneneri amachita

1. Kuyankhula mwa satanetsatane—Kuphunzitsa Baibulo, monga Ndili pano, ndi udindo wao waukuru, ena mwa aneneri a m’Baibulo ngati Yona sadalotsere za kutsogolo.

2. kulotsera—kunena za kutsogolo. Ulosi wotchuka pakati pao kunali kudali kuyang’ana kubwera kwa Yesu, kumbukirani kuti sadaone zonse zobwera mtsogolo kotero nthawi zambiri samatha kunvetsetse za ulosi womwe akunena. Dan. 12:8-9.

Aneneri ndi mabuku omwe samawerengedwe kapena kuphunziridwa kwambiri m’Baibulo. Abusa ndi aphunzitsi ambiri a Baibulo saphunzitsa kwambiri mabuku a aneneri. Ndikukhulupirira kuti izi zimachitika pazifukwa ziwiri izi. Choyamba ndichakuti uthenga wa aneneri ndi ovuta kuulandira chifukwa umachenjedza za chilango chifukwa cha kuchimwa kwa anthu. Chifukwa china ndichakuti uthenga wa aneneri ambiri ndiovuta kuunvetsetsa. Mauthenga a neneri amenewa amafuna kuwawerenga bwinobwno kuti

ukwanitse kuwaphunzitsa. Muli zambiri zomwe tingaphunzire zokhudzana ndi moyo wathu wa tsiku ndi tsiku.

Pamene mukuphunzira buku la mneneri mukuyenera kudziwa nthawi yomwe zochitika za bukuli zinalembedwa, komanso malo amene kumachitikira zinthuzi ndi yemwe akuyankhula mbukuli. Nthawi zina zimakhala zovuta kudziwa malo omwe ndi nthawi. Ena ngati Yeremiya timadziwa kuti adali mneneri ku Yuda ndipo amachita uneneri wake Yerusalemu atangotsala pang'ono kuti apatsulidwe ndikutenga anthu kupitanawo ku ukapolo ku Babulo.

Zoona zokhudzana ndi aneneri

1. Pali aneneri ambiri omwe sitikuwadziwa ndiponso Baibulo silidawatchule maina awo, koma akungokambidwa monga 1Samueli10:5. Iwotu adali ambiri m'Baibulo.

2. aneneri ena akutchulidwa m'mabuku otsiyanatsiyana. Eliya akupedzeka mu buku la1Mafumu. Ena ngati Elisa, Natani ndi Mose akutchulidwa mkati mwa mabuku otsiyanatsiyana a m'Baibulo palibe wa awa adalemba buku lake lake.

3. Ena adalemba mabuku omwe amadziwika ndi mayina awo monga Yesaya, Yeremiya (Maliro), Amosi.

4. Ena amatchedwa aneneri akuru chifukwa adalemba mabuku ataliatali, monga Yeremiya ndi Yesaya.

5. Ena amatchedwa aneneri a ang'ono chifukwa adalemba mabuku ochepa monga Mika, kapena adalembedwa mu Buku laochepa monga Yona.

6. uthenga wa mneneri aliyense ndiofunikira posawerengera kuti adalemba buku laling'ono kapena lalikuru.

7. Mungadziwe bwanji kuti mneneriyu ndionama? Timadziwa kuti mneneri ndioona ngati zomwe amalotsera zakwaniritsidwa.

A. Kodi uthenga wake ukufana ndi Baibulo? mneneri woona sadzatulutsa uthenga womwe uli wotsutsana ndi Baibulo. mwachitsanzo, mneneri woona sadzanena kuti ali ndi vumbulutso ndikulolera inu kuti mutaye lamulo la Baibulo nthawi ina iliyonse.

B. Kodi maulotsi ake akukwaniritsidwa? Pali zilango zokwana 7 kwa aneneri onama onani Deutronomo 13:5 kapena 18:20.

Mauthenga a aneneri nthawi zina ndiovuta kuwanvetsetsa, ndipo nthawi zina palibenso chomwe umanvapo. Ndichifukwa chake nthawi zambiri akhristu samawaphunzira. Nthawi zambiri amafuna kuima chamuna kuti uwanvetsetse, changuchi chimangochitika mwa kanthawi kochepa. Yembekedzani kuyamba kuwanvetsetsa mwa pang'onopang'ono pamene mupitilidza kuwawerenga kawirikawiri, ndipo mutsayembekedzere kuwanvetsetsa iwo mwa kanthawi kochepa zomwe amafuna kuti atanthaudze. Monga momwe mumachitira ndi mabuku ena onse, chitaninso chimodzimodzi ndi aneneriwa popempha Mzimu Woyera kuti ukuthandidzeni kunvetsetsa uthenga wawo. Mulungu amayankhula nafe motani? Lero Mulungu amayankhula nafe kudzera mu malembo ake Baibulo. Tsogolo lomwe tingalinene kuchokera m'Baibulo ndilakuti , Yesu akubweranso kachiwiri ndi chipambano cha chikuru.

Tilibe aneneri olotsera za ntsogolo matsiku ano Chibvumbulutso 22:18-19/ Deutronomo 4:2.

Ziphunzitso zotchuka za mauthenga a aneneri.

1. Udindo wathu mumapangano—kunvera Mulungu=kumbukirani kuti Mulungu ndi ndani ndizonse zomwe wachita=akuuzidwa kukumbukira Mulungu m'moyo wao. Uku ndiye kuphunzitsa.

A. Aneneri amaudza anthu kutsiya tchimo monga kupembedza mafano ndikubwerera kwa Mulungu, komanso ku Mau ake.

B. Aneneri amaudza anthu kuti akumbukire kuti Mulungu waapatula kotero kuti akuyenera kukhala moyo woyera. Akuyenera kuchitira umboni kupatulidwa kwawo.

C. Anthuwa akhale pa ntendere ndi anzawo. Phunzira la mpingo matsiku ano.

2. Phunziro lina ndi la Tsiku la Ambuye. Izi zimanena za chitsilidziro cha zinthu zonse, nthawi ya chiweruzo. Muli mfundo ziwiri muchiganizochi;

A. Chiwerudzo cha Mulungu kwa anthu otsakhulupirira—kutsindika kuti tchimo lotsalapidwa lidzalangidwa kwa muyaya.

B. Chipulumutso ndi cha anthu a Mulungu amene adzayeretsedwe ndipo osakhulupirira adzachotsedwa.

Tsiku la Ambuye lidzabwera ndi chiwerudzo kwa anthu ochimwa ndi mphoto kwa anthu okhulupirika.

3. phunziro lina lofunikira ndi lingaliro la Mesiya (kubwera kwa Mpulumutsi)—mau a chihebri amatanthaudza Ozozedwa. Kutanthaudza kuti wopatulidwa monga akulu a mpingo.

A. Pali maulosi ndi malongotsoledwe ambiri okhudzana ndi Mesiya muzolemba zokhudzana ndi aneneri. Tinganvetsetsa za kulongotsoledwa kwa Yesu muzolemba za aneneri.

Ulosi onena za Mesiya: Tanthaudzo

Mau oti "Ulosi onena za Mesiya" amatanthudza kuikidwa pamodzi kwa zolotsera zokwana 100 mu chipangano chakale zokhudzana ndi Mesiya. Ndizonveka bwino ndipo palibe angazikane nkhakhale kuti mauneneli amenewa adalembedwa ndi olemba ochuluka m'mabuku otsiyanatsiyana kwa zaka zokwana 1000. Zolembedwa zimenezi zidaliko asanabwere Yesu Khristu.

Ulosi onena za Mesiya: kukwaniritsidwa kwake

Khristu adakwaniritsa maulosi a Mesiya olembedwa ndi alembi a mu Chipangano Chakale. Muwerenge maulosiwa ndi kuona ngati wina aliyense wayetsera kukwaniritsa maulosiwa! Luka 24:44 akuti "ndipo anati kwa iwo, 'Awa ndimauwo ndinayankhula nanu, paja ndinakhala ndi inu, kuti ziyenera kukwaniritsidwa zonse zolembedwa za Ine m'chilamulo cha Mose, ndi aneneri, ndi Masalmo."

Onani maulosi ali mmusiwa amu Chipangano Chakele ndi kukwaniritsidwa kwake mu Chipangano Chatsopano ndi Khristu:

- Azabwadwa m'Betrehemu (Mika 5:2 Mateyu 2:1; Luka 2:4-7)
- Kubadwa ndi Namwali (Yesaya 7:14 Mateyu 1:21-23) ngati Mbeu ya Abrahamu (Genesis 12:1-3; 22:18; Mateyu 1:1; Agalatiya 3:16) ngati wa fuko la Ayuda (Genesis 49:10; Luka 3:23, 33; Ahebri 7:14), ngati wa kumudzi wa Davide (2Samueli 7:12-16; Mateyu 1:1).
- Herolde apha ana ongobadwa kumene (Yeremiya 31:15; Mateyu 2:16-18)

- Kutengedw kupita ku Igoputo (Hoseya 11:1; Mateyu 2:14-15)
- Kulalikidwa za iye ndi nthenga wa Ambuye (Yohane Mbatizi) (Yesaya 40:3-5; Malaki 3:1; Mateyu3:1-3.
- Kuzozedwa ndi Mzimu Woyera (Yesaya 11:2; Mateyu 3:16-17).
- Kulalikidwa uthenga wabwino (Yesaya 61:1; Luka 4:14-21).
- Kuchita zozizwa (Yesaya 35:5-6; Mateyu 9:35).
- Kukonza mkachisi (Malaki 3:1; Mateyu 21:12-13)
- Kutumikira ku Galileya (Yesaya 9:1; Mateyu 4:12-16).
- Kulowa mu Yerusalemu ali paburu monga mfumu (Zakaliya 9:9; Mateyu 21:4-9).
- Kuzionetsera yekha ngati mfumu kuchokera paja panabwera lamulo lomanganso Yerusalemu (Danieli 9:25; Mateyu 21:4-11).
- Kukanidwa ndi Ayuda (Masalmo 118:22; 1Petro 2:7)
- Kufa imfa yodzichepetsa (Masalmo 22; Yesaya 53) kukanidwa (Yesaya 53:3; Yohane 1:10-11; 7:5,48) kuperekedwa ndi m'bale (Masalmo 41:9; Luka 22:3-4; Yohne 13:18) kugulitsidwa ndi masekeli a siliva okwana 30 (Zakaliya 11:12; Mateyu 26:14-15), kukhala chete pamaso paomususa (Yesaya 53:7; Mateyu 27:12-14) kunyozedwa (Masalmo 22:7-8; Mateyu 27:31), kumenyedwa (Yesaya 52:14; Mateyu 27:26), kulavulilidwa (Yesaya 50:6; Mateyu 27:30), kulasidwa m'manja ake ndi mapazi (Masalmo 22:16; Mateyu 27:31), kupachikidwa ndi akuba (Yesaya 53:12; Mateyu 27:30), kupempherera iwo omuzunza (Yesaya 53:12: Luka 23:34) kulasidwa mu nthiti (Zekaliya 12:10; Yohane 19:34), kupatsidwa vinyo osasa kuti amwe (Masalmo 69:21; Mateyu 23:36) sathyola mafupa ake (Salmo 34:20; Yohane 32-36), kuikidwa m'manda a wachuma (Yesaya 53:9; Mateyu 27:57-60), kupanga maere pazovala zake (Masalmo 22:18; Yohane 19:23-24).
- Kuuka kwa akufa (Masalmo 16:10; Marko 16:6; Machitidwe 2:31)
- Kukwera kunka Kumwamba (Masalmo 68:18; Machitidwe 1:9)
- Kukhala padzanja lamanja la Mulungu (Masalmo 110:1; Ahebri 1:3)

Buku la Yesaya

Yesaya ali ndi maulosi ambiri onena za mwasatanesatane zokhudzana ndi Yesu. Mulinso maulosi onena za kubwera kwa chiweruzo. Izi zimanena momwe a Israyeli adzagonjetseredwe ndi kulangidwa. Maulosiwa ndi onveka bwino ngakhale kuti amatenga nthawi yaikuru kuti zonenedwazo zichitike. Mwachitsanzo, zina la Koresi linagwiritsidwa ntchito monveka bwino zaka 100 iye asanabadwe. Yesaya 44:28.

Pamene mukuphunzira buku la mneneri, ndikwabwino kuwaika iwo m'malo momwe adachitikira, nthawi yomwe adakhalako, bola ngati zikudziwika. Mwachitsanzo, Yesaya adali mneneri wa kudziko la Ayuda mu nthawi ya mafumu ngati Uziya, Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya. Kumayambiriro kwa utumiki wake, Yuda adali akudutsa mu nyengo za chuma, ndipo nthawi zambiri anthu akakhala achuma amachoka pamaso pa Mulungu. izi ndizomwe zachitika kudziko la United States of America. Dzikoli ndilolemera kwambiri, ndipo limalemekedza Mulungu, koma pano chuma chidapangitsa Amereca, ndi maiko a ku Ulaya kutsiya Mulungu. pakutha pa nthawi ya Yesaya, chuma chonse chidali chitathanso, ndipo iyinso ndi nkhawa ya anthu aku America.

Mitu 39 yoyambirira ikunena kwambiri za machimo a anthu a ku Yerusale ndi maiko ozungulira. M'mawu ena chiweruzo cha Mulungu ndiwo uthenga waukuru mu ndime zimenezi. Ngakhale nthawi zambiri Mulungu ankagwira ntchito ndi Ayuda, koma nthawi zina ankachitanso ndi maiko onse kuti kudziwike kuti Iye ndi Mulungu wa dziko lonse.

Maulosi oyambirira a Yesaya ndi otchuka okhudzana ndi chenjezo kwa anthu onse. Tiyeni mwachidule tiphunzire mutu woyamba ndikuona za ndondomeko ya kaphunzitsidwe kwake.

1. Vesi yoyamba ikutionetsa satanetsatane wa komwe Yesaya amakhala ndi anthu omwe adagwira nawo ntchito.

2. Kenako tili ndi mndandanda wa ziweruzo zomwe Mulungu awasusa nazo anthu ake, ndi chilango chifukwa cha machimo awo. Werengani vesi 2-9. Mulungu akuudza anthu kuti akuchimwa. Tchimo lake ndilakuti aukira Mulungu ndikumutchera mbuyo. Zolemba zambiri za Yesaya ndi kuchenjeza anthu kuti asapembedze mafano; koma mmalo mwake apembedze Mulungu. Yesaya akuwaudza kuti Mulungu ndiosakondwera nawo. Yesaya adali munthu ophunzira bwino kwambiri, zinthu zomwe timadziona kawirikawiri muzolemba zake. Onani vesi 3 pamene amatonza anthuwa kuti ng'ombe ndi aburu ndi zanzeru popedza zimadziwa mbuye wao koma Israyeli akulephera kudziwa mbuye wake.

3. Vesi 10-15 Mulungu akuthirapo ndemanga kuti sakondwera ndi kupembeza kwa anthuwo chifukwa cha mitima yao yoipa. Mu vesi 15 Mulungu akuopsedza kuwachokera anthuwa. Ichi ndichiopsezo chachikuru kwambiri, ndipo tichite mantha pamene Mulungu akunena izi, mofanana ndi anthu athu komanso dziko lathu. Onani Mbiri 7:13-14 pamene Mulungu akuonetsa chomwe chingachitike pamene wachotsa dalitso lake pamalo komanso pamene wachoka pakati pa anthu.

4. Mu vesi 16-19 anthu akuitanidwa kuti alape ndikutsiya machimo awo natsatira Mulungu. onani mavesiwa ndikuona dalitso lalikuru lakuperekedwa pamene tatsiya machimo athu ndikutsata Mulungu.

5. Kenako kumapeto a mutuwu akunena kuti padzakhala padalitso pakati pawo. Uwu ndiuthenganso wofanana ndi ife lero.

Tiyeni tione chitsanzo china chauthenga wa Yesaya. Mutu 5:1-7 Mulungu akunena za munda wa mpesa umene adautsamalira kopotsa. Vesi 2 ikunena kuti Mulungu akunena kuti amayembekedzera kukolola mphesa zokoma koma m'malo mwake wakololapo mphesa zowawa. Kotero Mulungu ndionyatsidwa, chincho akuchotsa chitetedzo chomwe adachitsiya pamundapo (vesi 5) ndipo pa vesi 6 akuti azatumidza chiweruzo. Vesi 7 tikunva kuti apa Mulungu akunena zokhudzana ndi anthu ake. Ndipo kumapeto kwa mutu wonsewu akunena za chilango choopsa. Zindikirani kuti m'mutu uwu kutsiyana ndi mitu ina mulibe kuitana anthu kuti alape kenako kulandira madalitso. Mulungu sakupereka mwai wachiwiri kwa anthuwa. Ili ndi chenjezo kwa ife.

Yesaya ndiovuta kumunvetsa chifukwa mitu yambiri sili mundondomeko malinga ndi nthawi yomwe adanenera. Chitsanzo cha izi ndi mutu 6 omwe ukunena za kuitanidwa kwa Yesaya kuti akhale mneneri. Tingayembekedzere mutuwu kukhala oyambirira m'malo mokhala mutu wa chitsanu ndi chimodzi. Chifukwa chomwe chikupangitsa izi kuti zikhale ndichakuti, Yesaya amati akayankhula mau ake amalembedwa nthawi yomweyo ndikukamatidwa pakhomo pa khomo lolowera kuchipata kuti anthu awerenge. Kenako zolembedwazi zidasonkhanitsidwa ndi kusungidwa kufikira nthawi yomwe zidaikidwa pamodzi ngati buku. Nthawi zina izi zimapangitsa ntchito yake kuti ikhale yosasatidana mwandondomeko.

Mutu 6 ndi nkhani ya kuitanidwa kwa Yesaya ndi Mulungu kuti akhale mneneri. Tikuona mu vesi 5 kuti Yesaya adamuona Mulungu. kodi mukukumbukira phunziro lija pamene Mose adamuona Mulungu? kodi limatchedwa chiyani? Limatchedwa kuona chizilezile cha Mulungu, (Theophany) onani zina pa Exsodo 3:2-6. Tikuona kuyankha kwa Yesaya pamene adakumana ndi Mulungu pavesi 5. Kuyankha kwake ndi mmene tingayankhire pamene tikuganidza za Mulungu mmene timaganidzira za ulemerero wa kupedzeka kwake. Tikuyenera kugonjetsedwa ndi maganizo a kudabwitsa kwake ndi chiyero chake ndi kuipa kwathu.

1. Ziwani momwe Mulungu adamuyeretsera Yesaya ku machimo ake kuchokera mu vesi 6-7. Dongotsololi ndilofana ndi m'mene timachitira pamene tikupemphera, ndikuvomereza machimo athu. Nthawi yathu imapita pamene tilemekeza Mulungu molingana ndi momwe Iye alili, ndipo timamupempha kuti atisuke machimo athu.

2. Yesaya tsopano wakonzedwa ndi Mulungu, ndipo ndiokonzeka kuti Mulungu amupatse ntchito yomwe wamuitanira, ndipo Mulungu akumufunsa funso, lomwe amafunsa okhulupirira wina aliyense, onani vesi 8. Mulungu amafunsa aliyense wa mwa anthu ake kuti amutumikire Iye, ndipo yankho lomwe Yesaya akubwedzera kwa Mulungu ndi yankho lolondola kwambiri. "ndili pano munditume" Mulungu ali pantchito ndi nkhristu aliyense ndipo ntchito iliyonse ndiyofunikira kuphatikidzapo kukoyeretsa mpingo.

3. ndipo mbali yotsilidza ya mutuwu ikunena za phunziro lofunikira kwa ife pamene tikuwerenga kuti utumiki wa Yesaya sumalandira chipambano komanso udzakhala wanthawi yaitali. Yesaya adali mneneri kwa zaka zokwana 65. Mbiri ya Ayuda imanena kuti Yesaya adaphedwa ndi mfumu Manase pomudula pakatikati ndi mpeni wochekera matabwa. Mulimonse anthu sadachite chomwe Yesaya ankawalalikira kuti achite komwe kudali kusanvera Mulungu; koma Yesaya adakhalabe okhulupirika pamaso pa Mulungu.

Zotsatira pakukumana ndi Mulungu, Yesaya adadziwa chiyero cha Mulungu, munjira yopatulika zomwe timadziona muzolemba zake. Amagwiritsa mau akuti "Woyera wa Israyeli" maulendo okwana 25 pomulongotsola Mulungu. koyamba tikuona mauwa pa mutu 4. Chidziwitso cha chiyero cha Mulungu chomwe chidali ndi Yesaya ndi chinthu chomwe tiyenera kuchitengera. Timadzindikira za chiyero cha Mulungu pamene tikuwerenga ndi kuphunzira Baibulo. pamene tikudziwa Mulungu bwino lomwe, ndipamene tidzakhale tikunvetsetsa za kuyera ndi ungwiro wa Mulungu, komanso ndikuona uchimo ndi kuipiratu kwa ife ntundu wa anthu.

Mutu 19 ndi ulosi onena za Igoputo. Vesi 1 ndi 3 akunena kuti dzikoli ladzadza ndi mafano, za masenga ndi nyanga. Kotero Mulungu akupereka chilango. Mu vesi 16 tikuona anthu aku Igoputo akudzindikira Mulungu pamene akumuopa Iye (Masalmo 111:10). Tikuona vesi 8-21 kuti anthuwo adatembenuka mtima. Vesi 22 tikunva kuti Iye azachiritsa anthu pamene akhala ana ake. Mulungu mu vesi 25 akulengeza za dalitso kwa anthu ake a ku Igoputo. Mpingo woyamba udali wamphamvu ku Igoputo, ndipo mpaka pano ulipo omwe ulipobe kumeneko.

Pamuti 40 uthenga wa Yesaya ukusintha kuchoka pa kutsindikidza za chilango kuyamba kuyankhula uthenga wa chitonthodzo. Onani mutu 40:1. Apa Yesaya akunena za uthenga wa anthu omwe adzakhaleko zaka zakutsogoloko pamene azamangidwe ukapolo ndikudutsa mu mnsautso. Ganizo la Mulungu lakupereka chintonthozo likhale chilimbikitso kwa akhristu onse. Chitonthozo cha Mulungu, chimachokera ku ganizo lakuti, Mulungu ndu wamphamvu mokwanira kutonthodza anthu ake ndipo amatikonda kwambiri. Yohane 3:16-17. Ife akhristu tili ndi zifukwa zonse kuti tikondwere chifukwa cha ubale wathu ndi Mulungu.

Yesaya alinso ndi uneneri okhudzana ndi mathero adziko lapansi. Onani mutu 65:1-7 pamene Mulungu akulotsera kudzalanga anthu chifukwa cha kusanvera kwawo. Mutu 65:17-25 akunena za madalitso kwa anthu onvera. Werengani mutu 57 kuti muone anthu ndi tsoka lawo monveka bwino. Vesi 1-2 tikuonetsedwa ife akhristu kuti tiyembekedzere mtendere ndi mpumulo, pamene vesi 20-21 akulonjeza kuti sipajdzakhala ntendere kwa yense woipa.

Mutu 58 ndi mutu okhudzana ndi kulambira Mulungu. vesi 1-2 mulungu akukana mapembedzo a anthu chifukwa akufuna kupembedza Mulungu pamene akupitilira kupanga zoyipa.

Vesi 3-6 akutilangidza zokhudzana ndi kusala kudya. Mulungu akunena kuti adzakhala okondwa vesi 8-14, akunena Mulungu kuti adzakondwa pamene anthu akumupembedza Iye ndi miyoyo ya ngwiro.

Muli maulosi ambiri onena za Yesu mu buku la Yesaya.tikuona zinthunzithunzi za moyo, ndi kuzunzika kwa Yesu mu ulosi wolembedwa zaka 700 Yesu asanabadwe. Buku la Yesaya likunena za mmene khungu la munthu lingakhalire pokana zoona zokhudzana ndi Yesu. Ayuda amaphunzira buku limeneli, koma kumakana ulosi wokhudzana ndi Yesu. Maulosiwa ndi onveka bwino okwaniritsidwa ndi Yesu ndikuti aliyense owerenga buku la Yesaya akhale ndikuthekera kovomeredza Yesu ngati Mesiya. Tiyeni tione mwapang'ono maulosi amenewa.

1. Yesaya 7:14 werengani. Tikuona kuti namwali adzaima nakhala ndi mwana ndipo mwanayo adzatchedwa Emanuwelikutanthaudza kuti Mulingu ali nafe. Ndimangodziwa za munthu m'modzi yemwe anabadwa mwa namwali, ndipo ameneyu ndi Yesu. (Luka mutu 1)Yesu akukwaniritsa dzina la Emanueli chifukwa adali Mulungu ndipo adakhala pakati pathu ngati munthu.

2. Tiyeni tione za boma loipa ndi labwino. Mutu 9:1-7 akutifotokodzera za kulamula kwa Yesu makamaka poyang'ana vesi 6-7. Padzakhala boma lachilungamo. Yesaya 3:4-6 akulonjedza za boma loipa ngati mbali ya chilango.

3. Mutu 11:1-17 akunena za Yesu. Mphukira ya Jese mu vesi 1 akutanthaudza a bambo ake a Davide. Tikukumbutsidwa kuti Davide adalonjezedwa kuti m'badwo wake udzakhala mpaka kalekale. Yesu ndiye mbeu yake. Mphukira akutanthaudza mfundo yakuti mu nthawi ya Yesu ufumu siudzakhala ngati mtengo wautali chifukwa chakugwa kwa ufumu ndipo chomwe chasala ndi kanthambi kakang'ono komwe kakuyetsera kuti kaphukire kuchokera ku chisa.

4. chiyambi cha Yesaya mutu 42:1-7 tikupedza ndime yoyamba pa ndime zokwana zinayi zomwe zimadziwika ndi Nyimbo ya kapolo wokhumudwa, zomwe zimanena zinthu zokhudzana ndi Yesu Khristu. Vesi 2-3 akunena kuti Iye ndi wolamula wopambana. Vesi 6-7 akunena momwe adzachidzire akhungu kutanthaudza kuchiza kwa kuthupi, komanso apa akunena za kuchilitsidwa kwa khungu la muuzimu.

5. Mutu 49:1-7 ndi 50:4-11 palinso zinthunzi za Yesu ngati kapolo.

6. Mutu 52:13-53:12 tikuona kapolo ozunzika yomwe ndi ndime yodziwika mwa ndime zakunena za kapolo wozunzika. Tiyeni tione mofatsira ndimeyi.

A. Yesaya 52:13 tikuona Yesu kuti wakwezedwa ndipo adzaimitsa mafumu a dziko lapansi.

B. Mutu 53:1-3 akutiudza kuti Yesu adazunzika pokanidwa ndi anthu ndikunva chisoni komanso kuvutika m'maganizo.

C. Mutu 53:4-6 akutiudza kuti adazunzika chifukwa cha ife ndipo kuzunzikaku kudachokera kwa Mulungu.

D. vesi 7-9 tikunva kuti Yesu adavomeredza tsoka lake popanda kukanakana ngakhale kuti adali adali opanda uchimo kotero kuti adakumana ndi imfa m'malo mwathu. Yesu adali ndi mphamvu ndipo kupita kwake kwa pantanda adapita chifukwa cha chikondi chake kwa ife. Palibe yemwe akadalola kuudzidwa kuti afere anthu pokhapokha akadavomeredza zimenezi.

E. Vesi 10-12 akunena kuti Mulungu amene adamukhadzula adzamupatsanso mphoto. Kapoloyu adafikira ku chipambano kudzera m'moyo wa kuzunzika, chifukwa kuzunzika kumakwaniritsa pulani ya Mulungu. kuzunzika mpaka lero kumakwaniritsa pulani ya Mulungu.

Yeremiya ndi Maliro

Mneneri Yeremiya anabwera pambuyo pa Yesaya patatha zaka 60. Uthenga wake udali wonena za kubwera kwa chiweruzo cha Mulungu ku Yuda ndi ku Yerusalemu. Yeremiya amadziwika ngati mneneri olira chifukwa mtima wake udali osweka pamene amatula uhenga wa chiweruzowu. Yeremiya 9:1 ndi 13:15-17.

Zambiri mwa zolembedwa m'bukuli ndi zonena za Mbiri ya matsiku osiliza a ufumu wa ku Yuda. Mbali ina ya bukuli ndi Mbiri ya Yeremiya, pamene gawo linalo ndi ulosi wa Yuda. Bukuli ndi lotsokoneza chifukwa silidaikidwe mwa ndondomeko monga zinthu zidachitikali. Lili ngati buku la Yesaya, kuti uthenga umalembedwa ndikuikidwa penapake, kenako nthawi ina adatsonkhanitsa mauthenga onse ndikuwaika pamodzi motsawerengera kuti zinthu zidachitika nthawi yanji.

Adabadwa ngati wansembe koma monga ngati Mose sadafune kuchita zomwe Mulungu adamuudza kuti achite. Mulungu adamuudza kuti wamuitana kuti agwire ntchito imeneyo ndipo Mulungu adzamuthandidza ndi kumutetedza. Mulungu adatetedza moyo wake, koma Yeremiya adaikidwa mundende, adamenyedwa, komanso kutsala pang'ono kuphedwa. Ndichitsanzo kwa ife kuti pamene Mulungu watiitana kuutumiki wake tikuyenera kuyankha potsayang'anira zovuta zomwe tikakumane nazo. Cholipira cha utumiki ndi chachikuru kwambiri, chimakutengera ngakhale moyo wako.

Adatumikira ngati mneneri kwa zaka zopitirira 40 muulamuliro wa mafumu okwana asanu. Mfumu woyamba adali Yosiya yemwe adali oopa Mulungu pakati pa ena onsewo; koma ena onse adali oipa pamaso pa Mulungu. adali mneneri pamene Yuda ndi Yerusalemu adagonjetsedwa ndi Babulo. Iyi idali nthawi yovuta ya Yerusalemu chifukwa anthu a ku Babulo adali a nkhaza ndipo Yeremiya adakonda anthuwo.

Yuda panthawiyi adalibe ufulu wodzilamulira yekha ndipo amakhalako pansi pa ulamuliro wa mafumu a ku Babulo ndi ku Igoputo. Mafumu onsewa adamenyana kuti alamulire Yuda. Chifukwa chomwe Israyeli lidali dziko la mphamvu komanso la chuma munthawi ya Solomo ndikuti Mulungu adaika pa iwo m'dalitso wake. Mu nthawi ya Yeremiya, machimo a Yuda adapangitsa Mulungu kuchotsa dalitso lake la chitetezo. Izi zikutanthaudza kuti Yuda ndiofoka kuti kotero sangaziimire pa Yekha.

I. Yeremiya mu ualamuliro wa mfumu Yosiya. 640-609BC 2Mbiri 34-35:27

1. patatha zaka zisanu chiyambire ntchito yake ngati mneneri, buku la chilamulo lidapedzeka mu kachisi. 2 Mafumu 22:8. Izi zidapangitsa chitsitsimutso mu dzikoli, ndipo Yuda adayambanso kulambira Mulungu pamene amalamulilidwa ndi mfumu yoopa Yehova Yosiya. Yeremiya adachenjedza kuti chisisimutso chingakhale chopindulitsa, ngati anthu asintha mitima yao ndikuyamba kupmbedza Mulungu. Yeremiya 2:22.

2. Buku la lamulo silidataike kwanthunthu; koma kuti silimatsatilidwa. Izi ndi zofana ndizomwe zimachitika ndi Baibulo m'masiku a Martin Luther. Baibulo lidangokhala ndi anthu ochepa chabe, koma ziphunzitso zake sizimatsatidwa ndi anthuwa. Mpingo udapanga njira zao za kapembezedwe. Pamene Martin Luther adawerenga Baibulo, adayambitsa mpingo wa Lutheran, wotsiyana ndi chikatolika, womwe umasutsa zina zamuchikatolika. Mfumu Yosiya atangomwalira, pambuyo pake padabwera mafumu woipa, ndipo Yuda adatsiya kupembedza Mulungu woona. Izi zikungoonetsa kuti anthu sadanvere Yeremiya pamawu ake akuti mitima yao ikhale yotsinthika. Amapembedza Mulungu m'maonekedwe, koma mitima yao idali yoipa.

II. Mafumu atatu olamulira Yuda kuchokera 609 BC mpaka 597 BC.

1. Mfumu yoyamba idali Jehoahazi amene adakhala mfumu kwa miyezi itatu, kenako adatengedwa ukapolo kupita ku Igoputo, omwe udali ufumu wamphamvu muderali panthawiyi. Yeremiya amakakamizidwa kuyankhula zinthu zoipa zomwe mfumu ndi anthu ankachita. Ndikoopsa kuyankhula motsutsana ndi mfumu, koma nthawi zambiri, Yeremiya amakakamizidwa kuchita zimenezi m'masiku antsogolo. Ngakhale mneneri Ezekieli adanenerapo za kugwa ndi kumangidwa ukapolo kwa mfumu Yehoahazi. Ezekieli 19:3-4

2. Mfumu yotsatira adali Yehoiakimu, ndipo iyenso adali woipa. Adaikidwa kukhala mfumu ndi ulamuliro wa mfumu ya ku Igoputo pamene adachotsa pampando mfumu Yehoahazi. pamene Yehoahazi adali mfumu, Igoputo ndi Babulo adamenyana nkhondo yomwe Babulo idapambana, ndipo Babulo adakhala wa mphamvu muderali m'malo mwa Igoputo. Izi zidali zofunika kwa Yuda chifukwa adali ofooka ndipo amayenera kulamuliridwa koyamba ndi Igoputo kenako Babulo. Babulo adatenga akapolo ndi chuma chambiri kupita nawo kudziko lakwawo. Mneneri Danieli ndiye m'modzi mwa akapolowa.

A. Yeremiya ngati mneneri, adachenjeza anthu kuti uchomo wao udzawapititsa ku chionongeko.

Mulungu kudzera mwa Yeremiya, adaitana anthu kuti alape, kotero kuti akawadalitse iwo. M'malo mwake anthu adapitilidza kuchimwa, ndipo m'malo mopita chitsogolo anthu ankabwerera m'mbuyo werengani Mutu 7:23-24.

B. Mulungu amadana ndi mafano komanso kusalongosoka kwa Ayuda, ndipo anagwiritsa ntchito Yeremiya kuzuzula a busa ndi aneneri onama amene amapotoza anthu. Mutu 23:1-2 ndi 27:9-10.

atsogoleri ndi aneneriwa adali okwiya ndi uthenga ya chionongeko wa Yeremiya ndipo adalamulira kuti Yeremiya aphedwe. Mutu 26:20-23 chiopsezo cha imfa ya Yeremiya chidakula popedza mneneri mzake dzina lake Uriya adaphedwanso. Mutu 26:20-23.

C. Yeremiya anenera za imfa ya mfumu Yehoiakimu. Mutu 22:18-19.

3. Mfumu Yehoiakimu adakhala mfumu kwa miyezi itatu. Adali mfumu yoipa kwambiri ndipo Yeremiya adalotsera za iye kuti adzatengedwa ngati mkaidi kupita ku Babulo. Izi zidachitika ndipo adakhalabe mkaidi, m'Babulo kwa zaka 37 (Yeremiya 22:24-30 ndi Ezekieli 19:9).

IV. Mfumu yotsilidza adali Mataniya, amene mfumu Nebkadnezzar anamutcha dzina loti Zedekiya. Ezekieli 17:12-13 akunena momwe Yuda adakhalira pansi pa Babulo chifukwa tikunva kuti Nebkadnezzar ndiyemwe adaika mfumu Zedekiya paudindo.

1. Mulungu kudzera mwa mneneri Yeremiya adaudza anthu kuvomeredza kukhala pansi pa Babulo kwa zaka 70 (Yeremiya 29:10). Mutu 51:59 akunena kuti Zedekiya adapita ku Babulo kukatsindika za ukulu wa Nebkadnezzar.

2. Patapita zaka 5, Zedekiya mopusa sadanvere Mulungu ndipo adaukira mfumu ya ku Babulo. M'mbuyomu adalonjedza kwa Nebkadnezzar pakulumbira pamaso pa Mulungu kuti sadzagalukira mfumu ya ku Babulo (2 Mbiri 36:13 ndi Ezekieli 17:13-21).

3. Kuukiraku kudapangitsa Nebkadnezzar kuononga Yuda komanso kulimbana ndi Yerusalemu. Mfumu Zedekiya akufunsa Yeremiya ngati angapambane pamaso pa mfumu ya ku Babulo. Yeremiya adaudza anthu kuti achoke ku Yerusalemu ndikukazipereka kwa Nebukadzzar chifukwa nkhondoyo izamulaka. Adamuudzanso Zedekiya kuti akadzipereke kwa Nebukadnezzar chifukwa Yerusalemu adzaonongedwa (Yeremiya 21:9-10).

4. Uthengawu omwe udali osatchuka udapangitsa Yeremiya kuponyedwa mzenje la matope (Yeremiya 38:6). Vesi 13 akunena kuti adapulumutsidwa ndi mphamvu za munthu wina wa ku Itiopiya.

5. Awa adali mauthenga onvetsa chisoni onena za chiweruzo cha Mulungu ku Yerusalemu. Ndi chilango chankhaza, koma Mulungu akuonetsabe chikondi chake pa anthu popedza anapatsa mau a chitonthozo kupita kwa anthu ake kudzera mwa mneneri Yeremiya (Yeremiya 30:18,22 ndi 31:3). Phunziro kwa ife ndilakuti ndikwabwino kupereka chidzudzulo kwa munthu yemwe timamukonda, koma tikuyenera kuwakumbutsa kuti timawakondabe ndipo chilangochi ndi phindu la iwo eni. Mulungu akuudza anthu, kuti chitatha chizuzulochi, adzabwedzeretsa anthuwa ku Yerusalemu (Yeremiya 29:10).

6. Anthu a ku Babulo adaononga mzindawo ndi kachisi. Anthu ambiri adatengedwa kupita ku Babulo ngati akapolo. Yeremiya adatsala mu nzindawu kufikira pamene adakakamizidwa kupita ku Igoputo komwe anakafera.

V. Bukulinso ngakhale muli zinthu zonvetsa chisoni komanso muli ndime zomwe zikunena za ulosi wa Mesiya.

1. Mutu 3 chikuyamba ndikunena za nkwiyo wa Mulungu chifukwa cha mafano a anthuwa. Komabe, mu vesi 12 Mulungu akuitana anthu onse ku kulapa ndipo akuti adzachita nawo chifundo. Umboni wakuti azayang'ana ku mpoto ndi njira yomwe ,Mulungu adayankhula kuti chisomo chake chimaperekedwa kwa osala a mafuko khumi a kumpoto kwa Israyeli chimodzimodzi ndi Yuda.

A. Vesi 16-17 akunena za nthawi yomwe sitidzafunanso likasa la chipangano chifukwa Mesiya adzakhala ali pomwepo ndipo adzakwaniritsa chofunikira chilichonse.

2. Pangano (lonjezo) Latsopano likutchulidwa ponena kuti Israyeli lakhala dziko mu pangano ndi Mulungu kuchokera pa tsiku la Abrahamu pamene Mulungu anamulonjeza kudalitsa anthu onse kudzera mwa iye (Genesis 12:1-3). Paphiri la Sinai Mulungu adapereka kwa Ahebri pangano la chilamulo lomwe pakusanvera lidzawabweretsera matemberero pamene akadzamvera lidzawabweretsera mwa ngwiro adzalandira m'dalitso (Exsodo 24:7). Anthu sadanvere lamulo mwangwiro kotero izi zinabweretsa kwa anthu chiweruzo.

A. Yeremiya akuulula pangano latsopano lomwe ndilokwanira kuchikhululukiro cha machimo; kuti anthu akalandire chipulumutso. Yeremiya 31:31-34.

B. Pangano latsopano linalowa m'malo mwa pangano lakale (Ahebri 8:13). Moyo ndi imfa ya Yesu Khristu ndi madziko a pangano latsopano (Luka 22:20).

C. Pangano latsopano ndi pangano la chisomo. Yesu adachita ntchito yonse ndipo chipulumutso chikuperekedwa kwa ulere kwa anthu ake (Aefeso 2:8-9).

IV. Tanthaudzo la mauwa ku Moyo wathu

1. uthenga wochuluka wa Yeremiya ndi uthenga wa chiweruzo. Izi nthawi zina ndizodabwitsa chifukwa Yeremiya ndi munthu wodzindikira kwambiri. Onani momwe

adalilira anthu chomwe cjili chifukwa chomwe amadziwikira ndi dzina loti mneneri olira (Yeremiya 9:1 ndi 13:16-17).

A. Zaka 700 pambuyo pake tikuona zinthu zonga zomwezi kwa mneneri wina wotchedwa Yesu, amenenso analira kulilira anthu ake (Mateyu 23:37)

B. Yeremiya adanenera ulosi wina ovuta, koma ndi mau adziwika bwino a chisomo kuchokera kwa Mulungu. awa ndi mawu adziwika bwino a chikondi ndi chifundo chochokera kwa Mulungu (Yeremiya 29:11 ndi 31:3).

2. Kulalika za chiweruzo cha Mulungu.

A. Yeremiya adali mwamuna wa ulemu wake, komabe adalalikira mokhulupirika za kuopsa kwa chiweruzo cha Mulungu kwa anthu amene Iye amawakonda (Yeremiya 7:20,30 ,33-34). Chidzindikiro cha mtsogoleri wa chikhristu weniweni ndichakuti amakhala munthu yemwe amakonda anthu ake, koma amapereka chidzudzulo pamene kuli kofunikira kutero.

i. muli maumboni ambiri a mkwiyo, kunyatsidwa ndi kupsa mtima kwa Mulungu kutsiya ndi maumboni onena za chikondi chake komanso ubwino wake (Salmo 90:11).

B. Maumboni onena za kugahena ndi ku chilango chotsatha mu Chipangano Chatsopano amachokera kwa Yesu Khristu. Padali pamtanda pamen Yesu adalawa imfa ndi Hade chifukwa cha anthu ake. Timadziona izi mukulira komvetsa chisoni kwa Yesu, “Mulungu wanga, Mulungu wanga mwanditsiiranji ine?” (Mateyu 27:46)tikuyenera kunvetsetsa kuopsa kwa machimo athu, ndikuopsa kwa Gahena ndikuthokodza pa chipulumutso chathu chomwe timachipedza pokhulupirira Yesu.

3. Chikhalidwe cha mtima wa munthu pachilengedwe

A. Mtima wamunthu ndiochimwiratu (Yeremiya 17:9). Yesu adayankhula kuti tchimo lomwe lili mkati ndilomwe limachimwitsa munthu (Mateyu 23:27, Marko 7:21-23).

B. Munthu aliyense ndiwoipa ndipo waweruzidwa kale ndi tchimo lake lomwe likumulepheretsa kulowa mu Ufumu wa Mulungu (Aroma 8:7-8).

C. Tikuyenera kukhala ndi mtima watsopano kuti tikalowe mu Ufumu wa kumwamba (Ezekieli 36:26). Yesu adayankhula izi ponena kuti tikuyenera kubadwa mwatsopano (Yohane 3:5).

4. Kudandaulira osochera

A. Yeremiya anadandaulira anthu a mulungu kuti asagwe m’manja mwa Mulungu; koma kuti abwerere kwa iye nthawi itsanathe.

i. adaudza anthu a ku Yerusalemu kuti ndiochimwiratu mwina kuposanso Israeli ndipo Mulungu adalanga Israyeli pakulolera Asuri kuwakantha (Yeremiya 3:11).

ii. adawadandaulira anthu kuti abwerere kwa Mulungu, ndikulapa machimo awo kotero Mulungu adzachotsa pa iwo mkwiyo wake (Yeremiya 3:12-13).

iii. akuyenera kubwerera kwa Mulungu mofulumira nthawi isanathe. Mbira yoonongeka itha kukonzedwanso pamene ikadali yaiwitsi (Yeremiya 18:4-6). Mbiya siingapulumutsidwe pamene ili yokalamba, ndiyouma, koma itha kungophwanidwa. Ife, monga mbiya, titha kupangidwanso mwatsopano ngati nkhristu pamene tikadali ndi moyo (Yeremiya 29:13-14 ndi Yesaya 55:6-7).

5. Kukhala yekha

A. Nthawi zambiri Yeremiya amanva mkati mwake kuti wasala yekha. Nthawi zambiri muzathawidwa ngati simulalika uthenga otsangalatsa anthu. Yeremiya adakanidwa ndi

akubanja lake, anzake, atsogoleri, aneneri, ndi ansembe. Onse adamuchokera. Adamenyedwa ndi kuopsezedwa kuti aphedwa. Yeremiya adazunzika ngati mneneri wapambuyo pake adamuchokera. Adamenyedwa ndi kuopsezedwa kuti aphedwa. Yeremiya adazunzika ngati mneneri wapambuyo pake Yesu Khristu (Yesaya 53:3).

VII. Mathero

1. Yeremiya ali ndi machezo ochuluka kuchokera kwa Mulungu kupita kwa Ayuda. Mulungu adachita molekerera AYuda, adawachenjedza, kuwaopsedza ndi kuwadandaulira anthu akewa kuti asiye nkhalidwe lotsanvera Iye. Adachita izi kwa zaka zochuluka kwambiri. Mulungu ndiolekerera inde, koma kulekereraku kumakhala ndi malire, ndipo pamene waganiza abweretse chilango, chilangocho chimakhala choopsa kwambiri. Mulungu kuchokera mu nthawi ya Yeremiya sadasinthepo, ndipo tikuyenera kukhala ndi chidwi ku machenjezo amenewa.

Maliro

Bukuli ndi buku la chisoni chifukwa likulemba zokhudzana ndi maliro a Yuda. Bukuli ndi mndandanda wa ndakatulo za maliro zokonzedwa ndi Yeremiya amene amadziwikanso kuti mneneri okhumudwa. Ndi buku lonvetsa chisoni kwambiri m'Baibulo. Mulungu walanga kolimba anthu ake ndipo Maliro ndi chizindikiro cha chisoni cha anthuwa.

I. ndakatulo yoyamba: chionongeko cha Yerusalemu (Mutu 1:1-22)

1. Maliro mutu oyamba ndi kulira kwa chisoni poyang'ana kuonongedwa kwa mzinda wa Yerusalemu. Mzindawu wasanduka bwinja chifukwa machenjezo atabwera ambirimbiri, Mulungu wabweretsa chipatsuko chotheratu ku mzindawu. Chipasukochi ndi chachikulu, ndipo mzindawu wachitisidwa manyazi ndi kusamukidwa. Kulilaku tingakuyerekedze ndi kulira kwa mkazi wamasiye yemwe wataya mwamuna ndi ana ake ndipo tsopano alibe chiyembekedzo (Maliro 1:11). Izi zizakhala chimodzimodzi ndi munthu wina aliyense amene amanyozera machenjezo onse ndikusavomeredza Yesu kuti akhale mkhristu. Pamene amwalira ndi kupita ku Gahena, azalira pozinvera okha chisoni kuti sogolo lawo lonse lizakhala kuzunzika ku Gahena moyo wao onse.

2. Yeremiya akunena monveka bwino kuti chilangochi chachokera kwa Mulungu, ndipo chachitika chifukwa cha machimo ndi kusanvera kwa Mulungu (Maliro 1:8). Mneneriyu akuyerekedzanso kuti anthuwa akuvomeredza kuti ndiochimwa, ndipo Mulungu ndiolungama kwanthunthu pobweretsa chilangochi kwa anthuwa chifukwa cha kuukira kwawo.

3. Yeremiya akunena za kusangalala kwa adani awo chifukwa akumana ndi chionongekochi. Yeremiya adapempha chionongeko cha adaniwa, chifukwa nawo ndiolakwa pa kuchimwira Mulungu (Maliro 1:21-22).

II. Ndakatulo yachiwiri: mkwiyo wa chilungamo wa Mulungu (Mutu 2:1-22).

1. Ndizoona kuti chionongeko cha Yerusalemu chachitika ndi anthu a ku Babulo, iwo achita izi chifukwa Mulungu wa agwiritsa ntchito ngati atumiki ake kulanga anthuwo. Ndi Mulungu amene wapangitsa chipatsukocho (Maliro 1:1-6). Mulungu nthawi zina amagwiritsa ntchito anthu amene asali mwa Iye kuti akagwire ntchito yomwe akuifuna kuti igwirike, angakhale kukalanga anthu ake a mulungu. kumayambiriro adagwiritsa ncthito dziko la a Asuri kulanga ufumu wa kumpoto wa Israyeli. Yesaya adalosera kuti Mulungu adzagwiritsa ntchito Koresi kupulumutsa Ayuda ku ukapolo ndikuwabwedzeretsa iwo ku Yerusalemu (Yesaya 44:28 ndi 45:1).

2. Mulungu ali ndi zifukwa zokwanira zolangira anthu ake. Tsopano Yeremiya akufinsa anthu kuti alape ntchimo. Akupempha Mulungu kuti awakumbukire iwo kuti ndi anthu akebe, posawerengera machimo awo. Adapemphanso Mulungu kuti ayang'ane anthuwa ndi diso la chisomo komanso lachifundo (Maliro 2:19-20).

III. Ndakatulo yachitatu. Chisoni ndi chiyembekezo cha mneneri komanso anthu (mutu 3:1-66)

1. Yeremiya adazindikira mavuto omwe anthuwa adakumana nawo. Adalira chifukwa cha tsoka la anthuwo. Munthawi iyi ya mavuto adali ndi chiyembekedzo komanso chikhulupiriro pa Mulungu (Maliro 3:23-24).

2. Ngakhale panthawi iyi ya nsautso, Yeremiya adali ndi chikhulupiriro cha mtsogolo chifukwa Mulungu adali okhulupirika masiku a mmbuyomu, ndipo Mulungu walonjeza kuzachita mokhulupirika mtsogolomu. Yeremiya adazindikira kuti Mulungu sadali okondwera ndi chilango chomwe adapereka pa anthu, nthawi zina amachita zinthu ndi zifukwa zonveka bwino (Maliro 3:33).

3. Yeremiya adapitilidza kunena kuti anthu adalandira chilango chifukwa chakutsakhulupirika kwawo, kusanvera ndi kuukira Mulungu (Maliro 3:40-42).

IV. Ndakatulo yachinayi: Kuonongedwa kwa Yerusalemu (Mutu 4:1-22)

1. Yeremiya adalongotsola kuti athuwa adazolowera kukhala ndi ulemelero komanso chuma. Adachita izi poona momwe anthuwa adagwera chifukwa cha tchimo lawo (Maliro 4:1-22).

2. Yeremiya dalongotsola mavuto omwe anthu adakumana nawo, pamene Yerusalemu amaononedwa komanso pambuyo pa kugwa wa Yerusalemu. Adalongotsola kuti anthu amakhala ngati maliro oyenda. Yeremiya adalongotsola chithunzi cha chilango choopsa cha Mulungu. ili ndi chenjezo kwa anthu onse kuti machimo awo azawabweretsera chilango choopsa cha Mulungu (Maliro 4:2-8).

V. Ndakatulo ya chisanu: pempho la kubwedzeretsanso kwa Israyeli (mutu 5:1-22)

1. Anthu alapa machimo awo ndipo akupempha Mulungu kuti awapulumutse kumazunzo awo (Maliro 5:1). Mathero a bukuli akutsilidza popanda chitsimikidzo chilichonse chakuti Mulungu adzabwerera, koma chiyembekezo cha anthuwa chili pa Mulungu yemwe amuitana mukupempha kwawo.

VI. Khristu ndi Mpingo wake

1. Yeremiya ngati chinthuzi cha Yesu.

A. Yeremiya adalira pakuonongeka kwa Yerusalemu ndi anthu (Maliro 4:11, 13)

B. pambuyo pake patapita zaka 600 Yesu adalira chifukwa cha chiweruzo chomwe chikubwera pa Yerusalemu (Luka 19:21-33).

A. Ayuda kachiwiri adzalangidwa chifukwa cha machimo awo opitilira (Mateyu 23:37).

2. Palibe mavesi a chindunji omwe akunena za ulosi wa Mesiya mundimeyi, koma pali mavesi ochuluka omwe akunena za zithunzi za Mesiya

A. Maliro 2:15-16 kenako Masalmo 22:13 ndi Mateyu 27:39-44.

B. Maliro 3:8 ndi Mateyu 27:46

C. Maliro 3:14 kenako Masalmo 69:12 ndi Mateyu 26:57-68

D. Maliro 3:18 kenako Masalmo 69:21 ndi Mateyu 27:34

E. Maliro 3:30 kenako Masalmo 69:20 kenako Yesaya 50:6 ndi Luka 22:63-64

VII. Zomwe tikuphunzira mu bukuli pa moyo wathu wa tsiku ndi tsiku

1. Moyo opanda Mulungu

A. nyengo ya anthuwo alibe Mulungu idali yowawitsa kwambiri pakuti adalibe mpumulo, adalibe chakudya, komanso ntendere (Maliro 1:3 ndi 6 ndi 9) idali nthawi yoopsa kwambiri.

B. Ndimwa Yesu yekha momwe tingakhale ndi zinthu zonsezi (Mateyu 11:28 ndi Yohane 10:9 ndi Yohane 14:16-17.

2. Kukhulupirika kwa Mulungu

A. Ngakhale anthu akuzunzika kwambiri; koma chiyembekezo ndi chikhulupiriro chilipobe (Maliro 3:22-23).

B. Tikuyenera kudalira Mulungu ngakhale pamene tili mu nyengo zowawitsa kwambiri (Yesaya 50:10).

VIII. Mathero

1. Maliro ndi buku la chisoni choopsa zedi, ndi kupweteka kwakukuru; koma angakhele panthawi yowawitsayi Yeremiya adalalikira za chiyero cha Mulungu, chilungamo chake ndi ukulu wake mu chiweruzo chomwe adachipereka pa Yuda. Njira ina yokambira izi ndi yakuti, Mulungu ndiolungama pamene adapereka chilango kwa anthu chifukwa cha ichi ndichimene chidali chowayenera. Anthu amene adzapite ku Gahena kwa muyaya azazindikira kuti akuyenera chilango chimenechi.

2. Palibe angazuzule Mulungu kut ndiopupuluma. Izi zidachitika pambuyo pa zaka zochuluka anthuwa akutatsidwa mobweredzabweredza machenjezo, ziopsezo, ndi mapempho kuti chilango cha Mulungu chigwera pa Yuda.

3. Angakhare munthawi ya msautso wao, tsogolo la chiyembekezo idalipobe (Maliro 3: 23).

4. Angakhale mau osiriza a Maliro tikuonabe kuti pali sogolo la chiyembekezo (Maliro 5:21-22).

5. Nthawiyi idali yopanda chiyembekezo, koma Yeremiya adakhulupirira malonjezo a Mulungu. Lonjezo la chipangano lomwe Mulungu adapangana ndi Abrahamu, Mose, Davide ndi Yuda silizaphwanyidwa. Yeremiya ali ngati Abrahamu; adakhulupirira motsayang'anira chiyembekedzo (Aroma 4:18). Palibe Kanthu kuti mukudusa munyengo yopanda chiyembekezo, palibe Kanthu kuti zikuoneka zosatheka bwanji, palibe m'dziko lapansi chomwe chingachotse okhulupirira pa chikhulupiriro cha mau a Mulungu. Koma Mulungu akhale woona ndimo anthu onse akhale onama (Aroma 3:4).

Ezekieli

Bukuli lidalembedwa ndi Ezekieli yemwe adali wa msembe komanso mneneri kwa Ayuda adakali ku Babulo ku ukapolo. Adabadwira ku Yerusalemu, ndikutengedwa kupita ku Babulo pa kugonjetsedwa kwa chiwiri. Adagwira ntchito mu nthawi yofana ndi Danieli komanso Yeremiya. Yeremiya adali mneneri ku Yerusalemu matsiku otsiliza kuti Nebukadnezzar aononge mzindawu. Nthawi yomweyonso Danieli adali mneneri ku Babulo maka ku bwalo la milandu la chifumu. Ezekieli ndi buku lovuta kulinvetsetsa zomwe zimapangitsa anthu ambiri kusaliwerengawerenga bukuli. Kuvutaku kukubwera chifukwa bukuli lazaza ndi zifanifani. Olembayu akugwiritsa ntchito, maso mphenya, ulosi, zizindikiro ndi zoyerekedza pochita zisuzo uthenga wa Mulungu. Izi zimapangitsa gawo lalikuru la bukuli kukhala lovuta kulinvetsetsa, koma mulu zoona zambiri zomwe zili zosavuta kuzinvetsetsa komanso zili ndi tanthaudzo kwa ife.

I. Gawo loyamba la bukuli likunena za kuikidwa kwa Ezekieli (1:1-3:27)

1. Mulungu adaonekera Ezekieli monga adachtira ndi Yesaya mmaso mphenya pamene Mulungu akuonetsa chithunzi cha ulemerero opotsa kwa aneneriwa. Tikuona kuyankha kwa Ezekieli ku zolongotsola za Mulunguzi komwe kuli kofanana pamene anthu atengedwa kupita komwe mulungu akupedzeka. Mutu 1:28 akutiudza kuti Ezekieli adagwa pansi pamene adaona ulemerero wa Mulungu.

A. Tiuyenera kuchita mantha pamene ,tikumana ndi mulungu, monga panthawi imene tikupemphera, komanso kuwerenga Baibulo (Yesaya 66:5). Kumbukkirani kuti mulungu ndi woyera ndipo ife anthu ndiozaza ndi uchimo.

2. Tsopano Ezekieli wachepetsedwa ndi Mulungu, ndiokonzeka tsopano kuimirira ndi mapazi ake kuti atumidwe ndi Mulungu. Adaphunzira kuti utumiki wake udzakhala ovuta monga zinkakhalira ndi aneneri en onse a Mulungu; ndipo adamupatsa utumiki wa magawo asanu.

A. Adapatsidwa mfunda wa dzina loti "Mwana wa munthu" lomwe lagwiritsidwa ntchito m'malo okwana 90 mubukuli. Mulungu atha kumalanga anthu ake koma sikuti waayiwala iwo, kotero watuma Ezekieli kwa iwo kukhala mthenga pakati pawo (Ezek.2:3).

B. Ezekieli adali ndi ulamuliro kuchokera kwa Mulungu, ndipo akuyankhula mau a Mulungu (Ezekieli 3:4).

C. Ezekieli adapedza mphamvu kuchokera kwa Mulungu. Tikuona izi pamene mulungu adamuutsa ku mapazi ake (Ezek. 2:2). Akapolo a Mulungu asayetserere kugwira ntchito ndi mphamvu zao. M'malo mwake tengani mphamvu zanu kwa Mulungu. Ezekieli akuphunzira kuti akagwira ntchito ndi anthu omwe auma mitima komanso kulimbana ndi iye kotero akakhala ndi utumiki ovuta kwambiri (Ezekieli 3:7-9).

D. Ezekieli akuyenera kukhala okhulupirika kwa anthu ake, Ayuda, angakhale anthuwa kadzakhala ovuta kwambiri (Ezek. 3:5, 11). Mutu 2 ukunena momwe anthu azakanire choonadi cha uthenga wa Mulungu monga adachitira ndi aneneri ena a Mulungu.

i. Phunziro kwa ife ndilakuti, tikuyenera kulalika mau a mulungu mokhulupirika ngakhale anthu akutikana komanso kukana uthenga wathu. Tikuyenera kuchita izi ngakhale zitakhala kuti zikhoza kubweretsa chiopsezo ku moyo wathu. Tisalalikire mauthenga onena zinthu ngati nthanzi, chuma, kupedza bwino. Tiphunzitse ndikulalikira zokhazo zomwe zili m' Baibulo

E. Tikhale onvera Mulungu. Onani momwe Ezekieli adachitira pomvera mulungu ndi kudya buku lomwe lidali buku la chilamulo pamene adalamulidwa kuchita motere (mutu 3:1-2). Tikuphunzira kunvera Baibulo zomwe ndichimodzimodzi kumvera Mulungu.

3. Udindo wa munthu ndi uthenga omwe Mulungu adamupatsa Ezekieli 3:18, 20, 33:8. Mulungu adzachita nafe malinga ndi momwe tidachitira ndizomwe Mulungu adatiramulira kuti tichite. Mwachitsanzo mkhristu aliyense adaitanidwa kuti akhale ofalisa mau a Mulungu.

A. Tikuona ganizo ili lakuti Mulungu adzachita nafe malinga ndi zomwe tidachita mumaga wo ena a Baibulo. Paulo adanena zakukhala m'mavuto ngati salalikira uthenga wabwino (1Akorinto 9:16).

II. Gawo lachiwiri la bukuli, tikuona Ezekieli akunenera za chiweruzo chotsutsana ndi Yuda, asanagwe Yerusalemu (Mutu 4-27). Yeremiya adali ali ku Yerusalemu, pamene Ezekieli adali ku Babulo; onsewa amalosera zinthu zofana zotsutsana ndi Yuda.

Maulosiwa kwambiri amachenjeza za kubwera kwa chionongeko cha Yerusalemu chifukwa cha machimo a anthu.

1. Mulungu akulonjeza chilango choopsa kwa anthu osati chifukwa ndioyipa kwambiri, komanso chifukwa chakuti kuipa kwaoku kudali kopambana kupotsa maiko a anthu a mitundu omwe adawazungurira mutu 5:7-9.

2. M'maso mphenya, Ezekieli adaona ena mwa machimo amene adabweretsa chilango pakati pa anthu monga kupembeza dzuwa ndi nyama monga anthu a ku Aigoputo chaputala 8:10,14,16.

A. Ezekieli akupereka chithunzi chakuchoka kwa ulemerero wa Mulungu mu kachisi ndi mu mzinda.

i. Adaona likasa la chipangano cha Mulungu litakwera pa njinga kuti lichoke 10:9.

ii. Akuona ulemerero wa Mulungu poyenda kupita khomo la kachisi 10:4. Kenako udanyamuka kupita mbali ya kuchipata cha kumamawa 10:19. Kenako udatuluka kunja kwa mzinda nupita ku kuphiri la Oliveti 11:23.

iii. Ulemerero wa Mulungu udakhala patali ndi Ayuda kufikira mutu 43. Ulemerero wa Mulungu ukutanthaudza kuti pamene anthu akuyandikira kwa Mulungu, Mulungunso amabwera chifupi ndi anthu. Mulungu mwini ndi ulemerero wa Yehova. Limodzi mwa chiweryzo kapena chilango cha anthu adazunzika nawo ndichakuti pamene mulungu adachotsa madalitso ndi kupedzeka kwake kwa anthuwo.

B. Ezekieli amalumikidzana ndi anthuwa kudzera pakamwa komanso zizindikiro. Mutu 12:6 Ezekieli mwakufuna kwake adapereka msembe mntendere ndi chimwemwe cha umunthu wake. Adapitirira kutumikira ndi kunvera Mulungu pambuyo pa imfa ya mkazi wake mutu 24:15-18.

i. Ezekieli adaonetsa kuonongedwa kwa Yerusalemu pochita ngati adaliko pamene mzindawu umaonongedwa. Zochita zake mu chaputala 4:1-17 zikuonetsa mzindawu pamene umaonongedwa.

ii. Mutu 5 ukuyamba ndikuyankhula za tsoka lansogolo la mzika zokhala mu Yerusalemu.

iii. Adalongedza katundu wake ndi kuboola khoma zomwe zimafanizira ukapolo wa khwimbi la Ayuda Ezek.12:1-20.

C. Posakhalitsa ku Yerusalemu, mfumu Zedekiya amakhulupirira kuti ali otetedzeka chifukwa amaona kutsutsana pakati pa ulosi wa Yeremiya ndi Ezekieli. Yeremiya amati mfumu idzatengedwa ukapolo ku Babulo (Yeremiya 21:7). Ezekieli adati mfumu siidzaona Babulo (Ezekieli 12:13). Zonena zonse za aneneri awiriwa, zinali zoona chifukwa maso a mfumu Zedekiya adzakololedwamo asadatengedwe kupita ku Babulo, kotero adapita ku Babulo koma asakuona (2 Mafumu 25:7).

3. Mfumu Zedekiya adakhadzikitsidwa kukhala mfumu ndi Nebukadnezzara amene adapangana naye pangano kuti sadzachita mpanduko potsutsana ndi Nebukadnezzara. Koma Zedekiya sadasunge panganoli Ezek. 17:13-15. Kuukira kwa Zedekiya kudali tchimo chifukwa adalumbira pamaso pa Mulungu kuti sadzaukira Nebukadnezzara (2 Mbiri 36:13).

4. Tikuphunzira mubuku la Ezekieli kuti Mulungu adakhala okwiya ndi Israyeli kuchokera pamene adali ku Aigoputo kumbembedza mafano. Tikuphunzira kuti chifukwa chokhacho chomwe Mulungu adaonongera Israyeli ndi chifukwa cha ulemerero wake (Ezekieli 20:1-9).

A. Mulungu azalanga tchimo panthawi yake, ndipo saiwala.

B. Mulungu amatipulumutsa chifukwa cha ulemerero wake osati chifukwa cha kupindula kwathu ngakhale kuti timapinduladi (Yesaya 43:7; 46:13).

5. Mkazi okondedwa wa Ezekieli adamwalira chaka choyamba cha kuvutidwa kwa Ayuda (Ezek.24:2, 18). Mulungu adaulula kuti imfa iyi ndichidzindikiro chakuti Yerusalemu sadzazemba kuonongako (Ezekieli 24:16-24).

III. Chiweruzo cha maiko ozungulira (Ezek. 25:1-32:32)

1. Mulungu akulengedza za chiweruzo cha maiko ozungulira chifukwa amapembedza mafano komanso adatseka chifukwa cha kugwa kwa anthu a Mulungu. sadangosangalala chifukwa chakugwa kwa Yerusalemu; koma adathandidzira kuchitira chiwembu Yerusalemu.

2 Igoputo ndi dziko lomwe Mulungu alilange mwapaderadera. Izi zili chomwechi chifukwa Igoputo kwa zaka zambiri wakhala akubweretsa mavuto pa anthu a Mulungu. Igoputo adzakhalapobe ngati dziko koma opanda mphamvu (Ezek. 29:15). Mbiri ikuchitira umboni za ulosiwu chifukwa dzikoli lakhala likugonjetsedwa ndi kulamulilidwa ndi maiko ena, ndipo ngakhale lero sidziko lamphamvu pa chuma. Zoona zake dzikoli ndilosauka pansi pa ulamuliro wa boma loipa la chisilamu.

IV. Ulosi onena za kubwerera ndi kubwedzeretsedwa (Ezekieli 33:1-48:35)

1. Yerusalemu ndi kachisi zidaonongedwa mu 538 BC, ndipo anthu adalangidwa koopsa. Anthu adakana kunvetsera machenjezo omwe Mulungu adawapatsa kudzera mwa aneneri otsiyanatsiyana. Amakhulupirira kuti popedza ndi mtundu wa anthu osankhidwa ndi Mulungu, kotero Mulungu sadzawalanga kotheratu. Mutu 24:25-27 akunena za uthenga otsilidza wa Ezekieli wochenjeza anthu za kubwera kwa chiweruzo. Tsopano Ezekieli ali chete kwa zaka zitatu patangotsala pang'ono kuti kugwa kwa Yerusalemu kuze.

2. Pamene mzindawu unagwa anthu adazindikira kuti ngakhale adali anthu psankhidwa ndi Mulungu; adayenerabe kukhala onvera kwa Mulungu kapena kulangidwa, kenako Mulungu adatumidza uthenga olimbikitsa wa kubwedzeretsedwanso mutu 33:48.

3. Muli mauthenga ochuluka onena za momwe ulemerero wa anthu ungazabwezeretsedwe;

A. pakumvetsera machenjezo a mlonda wa uzimu ndi kulapa Ezek. 33. Lero tingaone izi kuti zikutanthaudza kumvetsera machenjezo a Mulungu pamene akulalikidwa ndi atumiki ake okhulupirika komanso Baibulo.

B. Pakuchotsa abusa onama ndi kutsata Mbusa Wabwino (Yesu) amene ati adzabwere kuzatsamala khamu lake Ezek. 34. Uthengawu ungatanthaudze lero kuti tigwiritse ntchito Baibulo kuti tiziwe aphunzitsi ndi alaliki onyenga ndikuwachotsa. Tikuyenera kutsata aphunzitsi ndi alaliki okhawo amene amaphunzitsa zoona zokhudzana ndi Yesu ngati mutu m'Baibulo.

C. Pakupatsidwa mphamvu ndi Mzimu Woyera Ezek. 37.

D. Pakugonjetsa adani Israyeli Ezek. 38-39

E. Pakubwedzeretsa Israyeli kudziko lawo Ezek. 48

V. Khristu ndi Mpingo wake

1. Ulosi onena za kubwera kwa Mbusa Wabwino amene ali Yesu

A. Mulungu akuzitenga yekha ngati Mbusa Wabwino amene ati adzapulumutse anthu ake ndipo mwachikondi adzawatsamalira iwo Ezek.34:11-16. Timaona maumboni ambiri

onena za Mbusa amene ati adzatsamalire nkhosa zake. Yesu adazitcha yekha Mbusa Wabwino Yohane 10:11-16.

2. Ezekieli akuonanso za kchisi wa tsopano Ezek. 40-47, ndizoona kuti kachisi wa ku Yerusalemu adamangidwanso pamene Ayuda adabwerera ku Yerusalemu, ukapolo utatha, koma kachisi amene Ezekieli amalongotsola ndi kachisi opotsa yemwe Ayuda adamanga atabwerera ku Yerusalemu.

A. Kachisi yemwe Ezekieli amanena ndi chithunzi cha Yesu. Ndi chinthunzi cha nthawi ya Mesiya pamene akhala ndi ife.

i. Khristu ndi kachisi woona ndi wamoyo Yohane 2:19-22.

ii. Amawasonkhanitsa pamodzi anthu ake “miyala ya moyo” ndi “kumangidwa pamodzi ngati Nyumba yauzimu” 1Petro 2:5.

iii. Khristu ali m’modzi “mwa Iye chomangidwa chonse, ndichogwiridzana, kukula limodzi, ndikukula kukhala kachisi Woyera mwa Ambuye” Aefeso 2:21.

3. Mtsinje wa moyo ukuonedwa mu chaputala 47 kuti ukuyenda kuchokera mu kachisi. Uwu si mtsinje weniweni koma chitsanzo cha zinthu za uzimu. Uzabweretsa moyo pamene m’mbuyomu padangokhala imfa yokha. Izi zikuimirira Yesu Yohane 4:10.

4. Pangano la tsopno

A. Mulungu akufuna kupanga pangano lotsatha la mtendere ndi a Israyeli pambuyo pakubwerera ku dziko lawo Ezek. 37:26-28.

B. Tikuona chinthunzi cha chisisimutso cha uzimu pamene Mulungu adzaika Mzimu wake mwa iwo amene ali akufa mu uzimu Ezek. 37:1-14.

C. Mulungu akunena momwe anthu adzasinthire pamene apatsidwa Mzimu watsopano, wamnofu ndi Woyera.

D. Komanso ku Yerusalemu, mneneri Yeremiya akupereka uthenga ofanana panthawi ndi Ezekieli Yeremiya 31:33-34.

E. Ili ndi lonjezo labwino lochokera kwa Mulungu pamene akulonjeza kwa okhulupirira kukhala ndi Mzimu Woyera. Izi zimatsowekera ntchito yotheratu ya Yesu Khristu pa mtanda ndi kukwezeka kwake.

F. Madalitso oyamba mu Pangano Latsopano ndi awa:

i. Kuchotsa kwantunthu tchimo kupyorera m’mwazi wa Chipangano Chatsopano; pangano lotsatha Ezek.36:25 Yeremiya 31:34; Luka 22:20; Ahebre13:20.

ii. Lamulo la Mulungu lalembedwa mumtima watsopano; mtima wamnofu omwe wakhala pamalo pa mtima wa mwala Ezek. 36:26; Yeremiya 31:33, 2 Akorinto 3:3, 4:17.

iii. Mzimu Woyera wa Mulungu udzakhala mwa okhulupirira Aroma 8:9; 1Akorinto 3:16.

VI. Tanthaudzo la mauwa m’moyo wathu

1. Ezekieli akuphunzitsa kuti munthu aliyense adzayankha pa zonse zomwe akuchita. Anthu kuchokera pa Adamu ndi Hava, anthu awiri oyamba kulengedwa adayetsera kulodza zala pa wina ndi mzake patchimo lomwe adachita. Baibulo limatiphunzitsa kuti tikuyenera kuvomeredza pamachimo omwe tachita, m’malo moloza anthu ena kuti ndiamene apangitsa kuti tichimwe.

A. Adamu adayetsera kuloza Hava kuti ndiamene wapangitsa kuti achimwe, ndipo Hava adaloza njoka kuti ndiyomwe yamuchimwitsa Genesis 3:12-13.

B. Ganizola la udindo pa tchimo lomwe wachita likunenedwa pa Ezekieli 18:4,20. Palibe amene ali ndi udindo pa tchimo la munthu wina.

2. Mtima wa tsopano

A. Kuvunda ndi tchimo la Israyeli lachotsa chivomerezo cha Mulungu Ezek. 36:16-20. Palibe chomwe Israyeli wachita kuti alandirenso chikondi cha Mulungu.

B. Chomwe Mulungu akulonjeza kuchichita chidzachitika chifukwa Mulungu samafuna kuononga dzina lake koma osati chifukwa cha anthuwo apedza chisomo cha Mulungu ayi Ezek. 22-23.

C. Mulungu akufuna apereke mtima watsopano kwa anthu. Mtimawu udzadzala ndi chikondi kwa Mulungu ndi mzimu womvera Ezek. 36:25-27 ndi 11:19-20.

D. Lonjezoli lidakwaniritsidwa mu uthenga wabwino wa Ambuye Yesu Tito 3:3-6.

3. Obadwa ndi mzimu. Ezekieli wagwiritsa ntchito mau akuti Mzimu wa Mulungu ka 29, onani 2:2 ndi 3:12. Tikuona mwa Ezekieli kuti Mzimu Woyera ndiomwe umapangitsa kubadwa kwa tsopano (moyo wa uzimu) mwa anthu.

A. Nkhani ya chigwa cha mafupa owuma ikuonetsa ntchito yopambana ya Mzimu Woyera Ezek. 37:1-14. Iyi ndi nkhani yoonetsa kufa mu uzimu kwa Israyeli pansi pa chiweruzo cha Mulungu ndi kubadwanso kwa uzimu komwe Mzimu udzabweretse kwa iwo pamene Mulungu wabwedzeretsa anthu ake. Maso mphenyawa akuonetsa mavuto ambiri a a Israyeli pamene adali ku ukapolo. Imanena za kusasangalala kwawo pamene padalibe moyo wa uzimu.

i. Mafupawa adali ouma kwambiri zomwe zikuonetsa kuya kwa mavuto a anthu pansi pa chiweruzo cha Mulungu. mavuto enieni a anthu amadza pamene aukira Mulungu ndi Mau ake, pamene ali pansi pa ulamuliro wa tchimo, komanso kutheratu kewa chikhalidwe cha umunthu m‘mene iwo adagwamo.

ii. Mulungu adamulamula Ezekieli mu 37:4-5 kulalikira ndi kupemphera. Apempherere anthu akufa mu uzimuwo, Yohane 5:25 ndi kuitana Mzimu wa Mulungu kuti ulengenso ndi kuperekanso mphamvu Tito 3:5.

a. M’mawu ena Ezekieli adagwiritsa ntchito nkhaniyi ya chigwa cha mafupa ouma kuphunzitsa kuti ndi Mzimu Woyera ndiomwe umapangitsa kubadwanso kw akhristu. Mavesi a Chipangano Chatsopano ali pamwambawa akunenetsa za choonachi.

4. Akulu a mpingo akuzuzulidwa chifukwa cha kuzikonda ndi kutaya udindo wao, potsatsamala anthu Ezekieli 13:1-23. Atsogoleri adataya anthu awo potsawapatsa utsogoleri woyenerakotero anthuwa amwazika chifukwa adalibe mbusa Ezek. 34:4-5. Chimodzi mwa zolinga za ATA ndikuphunzitsa abusa kuti akhale atsogoleri abwino kwa anthu awo.

A. Tikuona mu Ezekieli kuti atsogoleri adali ndi udindo kuphunzitsa anthu awo zokhudzana ndi Mulungu ndikunveketsa bwinobwino machenjezo kwa ochimwa. Adayenera kutsamala anthu makamaka odwala, akazi amatsiye, ndi ana amasiye, monga amachitira ndi nkhosa zawo.

B. Utsogoleri mu mpingo wa Yesu Khristu ndiofanana chimodzimodzi. Atsogoleri akuyenera kulalikira uthenga wabwino ndipo anthu akuyenera kutsamalidwa mwachikondi Machitidwe 20:28, Akolose 4:17 1Timoteo 4:16 1Petro 5:2-4; Yakobo 3:1. Ganizira za machenjezo omwe aperekedwa kwa akulu a mpingo.

C. Ntchito ya Mbusa singayende moyenera popanda mtima wa mbusayo. Mukuyenera kuitanidwa ndi Mulungu kuti mukhale Mbusa kapena mkuru wa mpingo.

VII. Mathero

1. Mulungu adapereka ntchito kwa Ezekieli kuti akhutitse mitima ya anthu kuti ukapolo wao udzatenga nthawi ndi kukhalanso ovuta. Gawo loyamba la uthenga wake ndilokhudzana ndi chiweruzo cha Mulungu. uthenga wachisoniwu udasinthana ndi uthenga opereka chiyembekezo. Uthengawu udali owabwedzeretsa anthuwa kwawo ndikunena za chisomo cha Mulungu kwa anthuwa akalapa.

2. Ezekieli amagwiritsidwa ntchito kwambiri mu Chipangano Chatsopano, wagwiritsidwa ntchito ka 69 ndipo Chivumbulutso wagwiritsa ntchito bukuli ka 48. Ndizooneka bwino a Israyeli akubwedzeretsedwanso pakutha pa nthawi.

3. Ezekieli akunena za kubwerera kwa Mulungu kudzakhala ndi anthu ake 48:35.

4. Baibulo likuphunzitsa kuti pali mavuto akulu ndi chisoni pamene Mulungu wachoka pakati pa anthu ake Hoseya 9:12.

5 Kumwamba ndi malo abwino kukhalako chifukwa cha kupedzeka kwa Mulungu. kupedzeka kwa Mulungu ndikumene kumapangitsa mpingo ndi mmiyoyo yathu kukhala yopambana kwambiri.

6. Onani chithunzi chopambana cha kumwamba chomwe tili nacho chifukwa chakupedzeka kwa Mulungu Chivumbulutso 7:15-17.

Danieli

Danieli ndi mneneri ndi osilidza mwa aneneri akuruakuru ndipo adagwira ntchito nthawi yofanana ndi Yeremiya komanso Ezekieli. Adakhalako pa nthawi imene Yerusalemu adagonjetzedwa ndi kuonongedwa ndi mfumu Nebukadnezzara wa ku Babulo. Adali mnyamata wachichepere pamene adatengedwa kupita ku Babulo komwe adakakhalako moyo wake wonse. Danieli nkutheka kuti amachokera ku banja la ulemu komanso ophunzira bwino popedza awa ndiomwe adatengedwa ukapolo ndikutsankhidwa kukhala kubwalo la mfumu komwe Danieli adakatumikirako.

Danieli adakhala nthawi yonse ya ukapolo ndikuonerera kubwerera kwa Ayuda kupita ku Yerusalemu ngakhale kuti sadali nawo limodzi paulendowu. Adali munthu wa ulemu wake ndipo adakhala m'moyo omwe udali opanda chilema. Adali ngati Yosefe yemwe sadagwe mu tchimo loopsa. Iye ndi anzache atatu adaonetsa kuti ndikotheka kukhala okhulupirika kudziko lachilendo. Anthu ambiri omwe timawawerenga m'Baibulo kuti adatumikira Mulungu ndi anthu omwe panthawi ina yake anagwa m'mavuto a zaoneni. Onani moyo wa Abrahamu, Nowa, Davide ndi Mose.

Zinatheka bwanji Danieli kukhala ndi umboni wabwino wa Mulungu pamene amakhala kudziko la chilendo? Adachita izi pamene amaphunzira za Mulungu wake ndikukumana ndi Iye kawirikawiri. Adapemphera asadamatsulire maloto ndipo mutu 9 tikuona pemphero lalitali lomwe tikuyenera kuliphunzira ndicholinga chofuna kudziwa zambiri zokhudzana ndi kupemphera moyenerera.

Nkhani zophweka ndi zosavuta kuzinvetsetsa m'Baibulo zikupedzeka mubuku la Danieli. Mwachitsanzo, ana padziko lonse lapansi amadziwa nkhani ya Danieli ya kuponyedwa mzenje la mikango. Danieli alinso ndi maulosi ovuta kuwamvetsetsa. Danieli mwini wake samanvetsetsa ena mwa maulosi ake, ndipo mpaka lero ena amavuta kuti tiwamvetsetse.

I. Chiyambi cha chidule

1. Lidali khalidwe la mfumu Nebukadnezzara kulamulira akapolo ake potenga ena kukakhala kunyumba ya chifumu komwe amakaphunzitsidwa kuti adzakhale ogwira ntchito za boma.

A. Danieli ndi anzache atatu, adasankhidwa kukakhala kuchifumu komwe amakaphunzitsidwa za mabwalo a ku Babulo. Ababelo amafuna kutsintha anyamata achisozerawa kuchoka Chiyuda kukhala Ababelo achikunja. Chinthu choyamba chomwe adachita pofuna kusintha anyamatawa kudali kusintha mayina awo.

i. Danieli 1:6-7 pakati pa anyamatawa padali Danieli, Hananiya, Misayeli ndi Azariya akufuko la Yuda. Ndipo nkuru wa adindo adawapatsa maina ena; Danieli adamutcha Belitsazara; Hananiya adamutcha Sadrake; ndi Misayeli Miseki; ndi Azariya Abedinego.

ii. Ababelo adafunitsitsa kuti asinthe anyamata a zaka 14 kukhala Ababelo, amene azipembedza milungu ya chikunja. Maina awo akale amalemekedza Mulungu wao woona, koma maina atsopano amalemekedza milungu ya chikunja.

B. Danieli ndi anzache amakakamidzika kuima mwamphamvu ndi chikhulupiriro kuti akhale okhulupirikabe pamaso pa Mulungu. yetsero loyamba lidali chakudya chomwe amapatsidwa kuti adye. Danieli adafulumira kunvera Malamulo a chakudya omwe Mulungu adalamulira anthu ake kunvera kotero adafunsa kupatsidwa chakudya chomwe chidali chovomerezeka ndi Mulungu. Danieli adapepha kuti asakakamizidwe kudya chakudya chodetsedwa Danieli 1:6-16.

i. Mwaulemu Danieli adapempha kwa omwe amamuyang'anira ndikuwaudza kuti amuyang'anire kwa masiku khumi akudya chakudya chovomeredzeka ndi Mulungu kwa Ayuda. Mulungu adaonetsetsa kuti Danieli ndi anzake achite bwino ndi chakudyacho ndipo kwa matsiku khumi anyamatawo amaoneka athanzi kupotsa ophunzira ena.

2. Ichi chidali chiyambi cha maphunziro a zaka zitatu. Patatha zaka zitatu maphunziro awo adatha ndipo anthu anayiwa adapatsidwa mayeso ndi mfumu Danieli 1:19-20. Anyamata anayiwa adapedzeka kuti adali opotsa onse amene adaliko ngakhale m'mbuyomo.

3. Adasankhidwa kukhala m'maudindo akuruakuru, ndipo Danieli adakhala paudindo kwa zaka zokwana 70. Adakhalabe ndimphamvu angakhale pamene Babulo adagonjetsedwa ndi mafumu ena Danieli 1:21.

4. Anthu amenewa adali opambana kwambiri chifukwa pantchito zawo chifukwa adaopa Mulungu pachiyambi ndikumudalira kwa nthuthu. 1Samueli 2:30 amanena kuti iwo amene akulemekedza Mulungu, Mulungunso adzawalemekedza.

II. Zochitika zikuruzikuru m'moyo wa Danieli mutu 2:1-6:28

1. Mutu 2 ukunena za nkhani yoyamba ya zinthu zochitika zomwe zili zopereka chiopsezo kwa Danieli ndi anzache. Mfumu Nebukadnezzara adalota maloto omwe amamuopsa ndipo adafuna kudziwa chomwe amatanthaudza. Anzeru ake adalephera kumatsulira lotolo kotero adawaopsedza ndi imfa. Danieli adalowererapo, ndipo iye ndi anzache, adapemphera ndipo Mulungu adapereka tanthauzo la malotowo kwa Danieli.

A. Danieli 2:28-30, adapereka ulemu kwa Mulungu pomatsulira malotowa otsati kutenga ulemuwu kwa iye yekha. Ili ndi phunziro lofunikira kwa ife. Ndi Mulungu yemwe amapangitsa olalika Baibulo kukhala wabwino. Ndi mphamvu ya Mulungu yomwe imachilitsa anthu osati mphamvu zathu. Tikuyenera kudzichepetsa ndikuzindikira kuti chilichonse chomwe tikuchita chikuchitika mu mphamvu ya Mulungu osati mu mphamvu zathu.

B. Malotowo amanena za kubwera kwa ufumu wa kutsogolo pano pa dziko lapansi. Mafumu onse anayi adaonetsera kale mphamvu zake ndipo adatha kale. Ufumu wa chiroma ndi ufumu wosilidza mwa mafumu amenewa.

i. Mfumu wotsilidza, thanthwe mu 2:44-45 ndi ufumu wa muyaya wa Yesu Khristu. Ichi ndichinthun zi cha mphamvu mu m'Baibulo. onani Masalmo 118:22 kuti muone chinthunzi cha thanthwe kwanthawi yoyamba. Mwala umasonyeza kusatha/ kusasinthika/umuyaya.

C. Mfumu Nebukdnezzara ali okondwa kotero akukweza Danieli pa udindo wa pamwamba. Mfumuyi ngakhale pa vesi 47akuvomeredza Mulungu wa Danieli kuti ndi Mulungu wa milungu ndi Ambuye wa mafumu. Komabe monga amakhalira anthu ena amene akukhala mu chilango chotsatha, Nebukadnezzara sadatembenuke mtima ndi zimenezi. Akadalibe wa chikunja mu mtima mwake sadataye milungu ya chikunja ndikutembenukira kwa Yehova amene ali Mulungu woona ndi wa moyo. Kungoziwa Mulungu basi sikuli kokwanira, tikuyenera kukana milungu ina yonse ndikuika chikhulupiriro chathu chonse pa Yesu Khristu yekha pamene tilapa machimo athu kuti tipulumutsidwe.

2. Tikuona umboni wakuti Nebukadnezzara akadalibe wachikunja pa chaputala cha 3. Mfumuyi idamanga fano lalikuru kuti aliyense alipembedze. Anzache a Danieli adakana kuchita izi, kotero adaponyedwa mung'anjo ya moto momwe amayenera kufa. Koma Mulungu adateteza miyoyo yao, kotero pamene mfumu adayang'ana mu ng'anjoyo adaonamo amuna anayi (vesi 25). Uyu adali Yesu Khristu yemwe anadza kudzakhala ndi anthu ake ku zowawa zao. Yesaya 43:2 amatiudza kuti Mulungu wathu alinafe angakhale panthawi ya kuyetsedwa kwathu.

A. Kachiwirinso Nebukadnezzara, wachita chidwi ndi Mulungu, koma sadasinthe, adakhalabe onyada ndi wa mwano.

3. Tili ndi maso mphenya ena mu chaputala cha 4ndipo kachiwirinso ndi Danieli yekha amene angamasulire malotowa. Nebukadnezzara ndi munthu wamphamvu kwambiri padziko lapansi kotero ndi onyada kwambiri. Mulungu akuganiza kuti amupase phunziro.

A. Mulungu adamupanga kuti aziganiza ngati iye ndi ng'ombe kwa zaka zokwanira 7. Iyi ndi nthenda yeniyeni yomwe imapangitsa munthu kumazinva ngati iye ndi nyama. Dzina la matendawa ndi pachizungu ndi lekanfrope.

B. Phunziro apa kwa ife ndilakuti Nebukadnezzara adali munthu wozikweza kwambiri ndipo anazitengera ulemu yekha pazomwe adakwaniritsa. Mulungu adaganiza kumupatsa phunziro, ndipo anamupangitsa kuti azikhala ngati nyama pofuna kumutsitsa Nebukadnezzara kwa zaka 7.

C. Zikuoneka kuti nthendayi idachitikadi, chifukwa 4:33-37 akunena kuti patatha zaka 7 Nebukadnezzara adachira ndipo adalemekedza Mulungu ndipo adamupatsa Mulungu ulemu wonse chifukwa cha zomwe adakwaniritsa. Nthawi zambiri Mulungu amamutsitsa munthu ndi cholinga chakuti amupulumutse.

4. Patapita zaka 20 tikubwera ku mutu 5 nthawi ya ulamuliro wa mfumu yosilidza ya Babulo Belisezara. Zidaoneka zolembedwa pakhoma nthawi ya madyerero ndipo Danieli adaitanidwa kuti amasulire malembawa. Adalotsera kuti ufumu wa Berisezara ukutha posachedwa. Utsiku wa tsiku lomwelo, asilikali a Amedi ndi Aperisi adagonjetsa Babulo.

5. Mutu 6 uli ndi nkhani yodziwika ya Danieli mu zenje la mikango. Dariyo tsopano ndi mfumu ya Amedi ndi Aperisi. Nkhaniyi ndiyophweka kuiwerenga choncho tidzangopereka ndemanga zochepa. Munkhaniyi muli zinthu zofanana ndi nkhani ya Estere. Anthu onse awiri adali okondedwa ndi olamula, komanso onse adali ndi adani omwe amafuna

atawaononga. Amedi ndi Aperisi adali ndi lamulo lakuti pamene mfumu wangolamulira chinthu sangathenso kuchisintha. Munkhani zonse ziwiri mfumu adakhadzikitsa chilamulo, koma pamapeto pake adanong'oneza bondo ndi cholamulacho, pamene sadali kudziwa kuti chotsatira cha lamuloli ndi imfa ya anthu omwe adawakonda. Onse Estere ndi Danieli adakhulupirira Mulungu ndikukhala okhulupirika kwa Iye. Mu nkhani zonse ziwiri, Mulungu adapulumutsa akapolo ake okhulupirika ndikuononga adani awo. Ifenso tikuyenera kukhulupirira Mulungu ndipo Iye adzatipulumutsa, ngati sadzatipulumutsa ku imfa ya kuthupi, ndiyekuti motsakayikira adzatipulumutsa ku imfa ya uzimu.

A. Zotsatira za izi, Danieli adakondedwa kwambiri ndi mfumu, kotero adakwezedwa udindo omwe akadakhodza kutetedza a Israyeli.

III. Ndipo kwinaku bukuli likunena za maulosi otsiyanatsiyana kuonetsera zakuti Mulungu amalamulira maiko onse.

1. Zolemba za bukuli kuyambira pa chaputala cha 6 ndi zokhudzana ndi zinthu za ntsogolo. Uku ndi kulemba maulosi onena za kutsogolo ndipo kwambiri onena za nthawi yotsilidza. Zolemba za moyo wa ntsogolo zimapedzeka kwambiri m'mabuku ambiri m'Baibulo, monga buku la Yesaya, Yoweri, Zakaliya, Danieli, ndi Chibvumbulutso. Zolembazi zimachuluka ndi zizindikiro, maloto ndi maso mphenya zomwe zimapangitsa kuti zotere zikhale zovuta kuti tizinvetsetse.

2. Mutu 7 ukuyamba ndi maso mphenya a maufumu anayi. Muli zofana ndi loto lomwe lili muchaputala cha 2. Monga aonetseredwa mafumuwa, ufumu uliwonse, ndiwamphanvu kwambiri, ndioopsa kupotsa wapambuyo pake.

Panthawi ino chiweruzo chaonesedwa. Mipando ya chifumu yakhazikitsidwa m'mwamba, ndipo masiku a m'mbuyomo, adatenga mpando wake, ndipo zilombo zaweruzidwa. Maufumu onsewa anadusa ndipo otsilidza unali wa Aroma.

A. Danieli 7:8 akuyamba kunena za nyanga yaing'ono yomwe anthu ambiri amaganidza kuti iyi imanena za okana Khristu; munthu wosaweruzika 2 Atesalonika 2.

B. Pali kutsiyana kwakukuru maka pankhani ya kumasulira ndime zimenezi, koma zinthu zina sizivuta kuzinvetsetsa. Danieli adatukula maso ake kumwamba pamene amaona kusinthana kwa mipando ya chifumu zomwe zidatsatira Aroma kufikira kunthawi zotsilidza.

C. Pamene Danieli adatukula maso, Vesi 9-10, adaona ukulu wosatha mu ulemerero wake. Akuona Mulungu wamkuru amene adzagonjetse onse amene amalimbana naye. Mulungu adzachit chiweruzo.

D. Tsopano pa vesi 13 tikuona kupitirira kwa maso mphenyawa. Tikuona Yesu yemwe amaoneka ngati munthu. anenedwa chonchi chifukwa Yesu adali asanadze padziko lino lapansi ndipo wabadwa ngati munthu. Tikuona mu vesi 14 kuti Yesu akupatsidwa mphamvu mu ufumu wosatha.

E. Tikuona vesi 24-27 kuti nyanga yaing'ono kapena kuti wokana Yesu adzasagana ndi maufumu onse ndikukhala olamula. Mbiri yonse ikulunjika nthawi pamene nyanga yang'ona idzaima ndikukhala wamphamvu ndipo adzazunza akhristu.

Adzalamulira mwamwano,kufikira monga vesi 26 ikutiudzira kuti bwalo la kumwamba lidzamuchotsa pampando, ndipo akhristu adzapambana pa choipa. Vesi 28 akutiudza za kuvutika kwa Danieli ndizimene adaona koma adazisunga izi kwa iye yekha.

F. Maso mphenya mu chaputala cha 7 chikuunikira za mbiri ya dziko la mtsogolo. Zoipa zizakhala zamphamvu pamene zizapikitsane ndi Mulungu. akhristu azavutik ndipo mpingo

uzalowa pansi. Pachimake pa mphamvu za okana Khristu, Ambuye adzabwerera ndi chipambano chachikula kuzonse zoipa.

3. Tili ndi maso mphenya atsopano pa chaputala 8. Vesi 2 ikutiudza kuti Danieli adatengedwa ndi Mzimu ndikupita ku likuru la ufumu wa Perisiya. Maso mphenyawa akunena za maufumu omwe adali akutsogolo kumbali ya Danieli ndipo ndiakale kwa ife.

A. Danieli 8:9 pamene Danieli amaona nyanga zinayi adakhazikika pa nyanga yaing'ono. Nyanga yaying'ono zikutanthaudza kubwera kwa mphamvu za olamulira a anthu otchedwa akasidi amene adzalamulire Ayuda kwa zaka zokwana 400 pakatikati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Vesi 10-12 akunena za nthawi ya olamula wa nkhaza yemwe adzazuze Ayuda. Olamulira uyu adzakhala wankhaza zopotsa, ndipo adzaletsa Ayuda kupereka msembe ndi kulambira Mulungu wao. Olamuliyu, Antiokasi Epifanesi adabweretsa mukachisi milungu ya boza. Idali nthawi yowawitsa kwa Ayuda.

B. Danieli akuuzidwa mu vesi 13-14 kuti nthawi iyi ya masautso osasimbika idzatha zaka 6 ndi miyezi inayi, kenako kachisi adzayeretsedwa ndipo Ayuda adzayamba kupembedzanso kawiri moyenerera. Izi ndi zomwe zidachitikadi.

C. Kodi thanthaudzo la izi kwa Ayuda lidali lotani? Vesi 16 ikutiudza kuti mauwa adalamulira mngelo kulongotsola zinthu kwa Danieli. Mauwa atha kukhala Yesu chifukwa ndi Mulungu yekha amene angalamule Angelo.

i. Ulosiwu udali chisime cha chitonthozo kwa Ayuda amene adazuzika pansi pa Antiyokasi. Izi zili chomwechi chifukwa vesi 25 akuudza Ayuda kuti masautso adzatha. Adatsimikidziridwa kuti panthawi yoikika Mulungu adzachotsa owazunza.

4. Mutu 9:1-2 tikuona Danieli amawerenga Malembo Opatulika ndipo adawerenga lonjezo lakuti pamapeto pazaka 70 mayetsero a Yerusalemu azatha ndipo anthuwo adzabwedzeretsedwa. Adzabwerera ku Yerusalemu. Dziwani kuti Danieli ali ndi zaka 84 koma akuphunzirabe kuwerenga Baibulo.

A. Kuyankha kwa Danieli pa izi kudali kupemphera ndipo tikuona pa vesi 3-19 chitsanzo chachikuru cha momwe tingapempherere. Tiyeni tione zinthu zisanu ndi chimodzi zomwe tikuphunziramo;

i. Danieli adali ndi chidwi ndi pemphero lake.

ii. Chinthu chachiwiri ndi pempheroli tikuchiona pa vesi 3. Danieli adali chifupi ndi Mulungu, komabe Danieli amakhala ozipatula pamene amakumana ndi Mulungu.

iii. Pempheroli kwambiri limavomeredza kuti iye ndi anthu adachimwadi, ndipo lidali tchimo limeneli lomwe lidapangitsa Mulungu kuwapatsa chilango chowayenera. Akunena pa vesi 11 ndi 14 kuti Mose adalonjeza chilango pakusanvera kwa anthu.

iv. Danieli adabwera kwa Mulungu ndikukhulupirira chifundo chake. Tikuona izi pa vesi 4.

v. Amabwera pamaso pa Mulungu ndi chopempha china chake. Mwanjira ina, amamuudza Mulungu chomwe akufuna.

vi. Danieli amapemphera mwa chinsisi.

B. Pempheroli lidatsogolera ku vumbulutso lalikuru lomwe tikuliona mu vesi 20-27. Tikuwerenga kuti pempheroli lidanveka kumwamba pamene amapemphera ndipo Gabrieli adabwera ndi mayankho a mapemphero ake. Pali maganizo osiyana okhudzana ndi ulosi wa Gabrieli. Ili ndi limodzi mwa matanthaudzo a ulosiwu.

i. Vesi 25 akunena za kumanganso Yerusalemu munthawi ya Ezara ndi Nehemiya.

ii. Tikuona ulosi onena za Mesiya mu vesi 25

5. Mutu 10-12 ndi gawo limodzi lomwe lili ndi maso mphenya ovuta kwambiri.

A. Mutu 10 tikuona Danieli akulira chifukwa cha kubwera kwa masautso omwe anthu ake akuti akumane nawo.

i. Tikuona kuti padali nkhondo ya muuzimu yomwe idali kupitilira. Baibulo lonse timapatsidwa nkhani za dziko la uzimu lomwe lili ndi mphamvu zakuchita ubwino ndi mphamvu zotsutsana ndi Mulungu. Satana ndi ntsogoleri wa iwo amene amalimbana ndi kutsutsana ndi Mulungu.

B. Mutu 11 komanso mavesi 4 oyambirira a mutu 12 ali ndi maso mphenya omwe ali ndi magawo atatu. Ulosi umenewu umaonedwa motsiyana, ndipo 1 akunena za 1 opatulika kwambiri. Maso mphenyawa amanena za Mbiri (hisitole) kuchokera mu nthawi ya Danieli kufikira panthawi yomwe Agriki adzalamulire Israyeli mu nthawi yapakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano kwa zaka 400. Kenako masomphenyawa akuyang'ana ku zinthu zochitika m'matsiku osilidza yomwe idzakhale nthawi yowawitsa kwambiri ya masautso.

i. Gawo loyamba tikuliona mu vesi 1-19 Danieli amalosera zinthu zochitika mtsogolo kwa ana a Israyeli, koma kwa ife lero zinthu zimenezi ndi Mbiri chabe (hisitole). Zambiri mwa zinthu izi zidachika munthawi ya hisitole yomwe zaka 400 pakati pa Chipangano Chatsopano ndi Chipangano Chakale. Pophunzira Mbiri imeneyi zimaoneka kuti zoletsera za Danieli zidali zoona.

ii. Mbali ina ya ulosiwu ikupedzeka mu vesi 20-35 tomwe ikukhudzana ndi olamula oyipa otchedwa Antiyokasi Epifanesi amene adalamulira panthawiyi pakati pa Chipangano Chakale ndi Chatsopano. Akutchulidwa mu chaputala 8 ngati "nyanga ina". Ndi m'modzi mwa anthu omwe analowetsa mafano mu kachisi. Mbiri imanena zambiri zokhudzana ndi mtsogoleri ameneyu ndikutsimikidzira zonena za Danieli.

iii. Gawo lotsilidza la ulosiwu likupedzeka pa Danieli 11:36-12:4. Pali kutsagwiridzana pankhani ya tanthaudzo la ulosi umenewu. Kodi ndizoona kapena ndichifaniziro chabe? Kodi ndi Mbiri kapena ndizinthu zochitika mtsogolo kwa ife lero? Ndikuona ngati ndi zakutsogolo kwa ife chifukwa palibe chilichonse mumbiri chomwe chimaoneka kuti chidachitika ndi ulosiwu, komanso vesi 40 ikunena za nkhondo yomwe idzachitike pamapeto pa nthawi. Izi zizachitika Yesu akadzabweranso ndipo padzakhala nkhondo yotsilidza pamene Satana adzagonjetsedwa ndipo Yesu adzawina nkhondoyi.

C. Mutu 12:5-14 ukumalidza buku la Danieli. Mafunso afunsidwa koma osayankhidwa. Tikuona kuti pali zinthu zomwe Danieli akuleohera kuzinvetsetsa komanso ife sitikuzinva. M'mene zinthu zidzakhalire m'atsiku omalidza ndizinthu zovuta kuzinvetsetsa kwa ife.

D. Phunziro kuchokera mu Chaputala 12.

i. Gawo lotsilidza la vesi 4 likunena zokhudzana ndi m'mene anthu adzaphunzirire zambiri koma osanvetsetsa. Dziko lathu lero laona anthu akupita patsogolo ndi nzeru monga za sayansi, koma nzeru ikuperewerabe. Anthu anzeruwa akunyoza Mulungu. Miyambo 9:10 akunena kuti nzeru imachokera kwa Mulungu.

ii. Tikuona m'maso mphenyawa kuti kuipa kudazpitilira kukula nsinkhu (Danieli 12:7 ndi 10:11. Tikuona kuti choipa chikumangokulira kulirabe m'madera mwathu lero.

iii. Chinthu chotsilidza chomwe tikuchiona ndi njira ya chikungamo. Mfundo ya mutu 12 ndikulimbikitsa anthu Mulungu kupambana pa choipa. Timachita izi ndi chikhulupiriro chomwe timachiona mu vesi 9 chifukwa Mulungu saulula chilichonse kwa ife. Tikuyenera kukhulupirira chilichonse ngakhale chimene sitichinvetsetsa.

iv. Tikuona pa vesi 10 kuti masautso akuza ndipo pa nthawi ya masautso oopsa, olungama adzanvetsetsa kutsiyana ndi oipa. Palibe anganvetsetse vesi 11 koma vesi 12 ikutiudza kuti olungama panthawi yoyenera adzapatsidwa chidziwitso choyenerera ndipo tidzakhala okondwera kuti tinakhulupirira Mulungu ndikukhala okhulupirika. Vesi 13 ikutiudza kuti okhulupirika adzapatsidwa mphoto pamapeto pa zonse.

Tione aneneri ang'onoang'ono

Pali mabuku 12 omwe timawatcha mabuku a aneneri ang'onoang'ono. Tiona ochepa mwa awa chifukwa cha kuchepa kwa nthawi. Mabuku awa monga momwe alili aneneri akuluakulu, saphunzitsidwa kawirikawiri mmipingo. Chifukwa chake ena amati mabukuwa ndi ovuta kuwanvetsetsa. Chifukwa china ndichakuti uthenga wa aneneriwa ndionena za chiweruzo zomwe anthu ambiri safuna kukumbutsidwa. Izi ndizoipa kwambiri chifukwa muli ziphunzitso zambiri m'mabukuwa.

Hoseya

Ili ndi buku loyamba la aneneri ang'onoang'ono. Mabuku 12 amenewa akupezeka kumapeto a Chipangano Chakale m'Baibulo. njira yabwino yophunzirira mabukuwa ndi mabuku a aneneli akuluakulu ndi kuwawerenga pamodzi ndi mabuku onena za Mbiri omwe ali ndi zinthu zomwe zimachitika munthawi ya aneneriwa. Hoseya adali mneneri ku ufumu nwa kumpoto munthawi ya Mafumu wachiwiri mutu 14 kufikira mutu 17. Iyi idali nthawi ya kumapeto kwa ufumu wa kumpoto, pamene a Asuri adagonjetsa ufumu wa a Israyeli ndikusalaza ufumuwu.

Uthenga wa Hoseya ndiovuta kwambiri. Mulungu ndiokwiya ndi anthu ake chifukwa amutsiya iye ndiyamba kupembeza mafano. Adalamula Hoseya kukwatira hule, ndipo Mulungu adagwiritsa ntchito izi kuonetsa zomwe Israyeli adachita pamaso pa Mulungu. israyeli wachita chigololo posiya Mulungu amene adamukonda ngati mkazi wake ndikupereka chili chonse chomwe Israyeli amafuna. Tikuona izi zikuperekedwa mofanana ndmomwe Goma ankamuchitira Hoseya.

Hoseya adali ndi moyo wosautsika kwambiri. Adakwatira mkazi yemwe amamukonda ndi kumupatsa zomwe amafuna. Koma adaperekedwa ndi mkazi wakewake monga momwe Mulungu adakanidwira ndi anthu ake ake. Adakonda anthu a ku Israyeli, kotero uthenga wake ndiwotentha kwa iwo. Anthu amafunikira kulapa kuti apewe mkwiyo wa Mulungu koma sadatero. Komanso kupedzeka kwa ufumu wa kumpoto udayambika chifukwa chogalukira Mulungu, kotero ufumuwu udali wotsayenera kotero sukadakhala oona kwa Mulungu.

I. Gawo loyamba la bukuli, banja la Hoseya ndi chizindikiro cha ubale wa Mulungu ndi Israyeli (Mutu 1-3).

1. Nkhani ya kusakhulupirika kwa Goma pamaso pa Hoseya yakambidwa ndipo ndiyofanana ndi nkhani ya kusakhulupirika kwa Israyeli pamaso pa Mulungu. Mulungu amasamala ndi kukonda Israyeli monga Hoseya amachitira ndi Goma. Israyeli adapita kwa milungu monga adachitira Goma kuyenda ndi amuna ena. Koma Hoseya adabwedzera mkazi wake komwe adapita, chimodzimodzi Mulungu yemwe adzapulumutse anthu ake ku mavuto awo.

II. Chiweruzo chikuperekedwa motsutsana ndi Israyeli. Gawo ili, mutu 1-3 mwachiziwikire, ndi chidule cha chiphunzitso cha Hoseya kwa zaka 40 chonena

zokhudzana ndi tchimo la Israyeli komanso chilango chomwe chikubwera pambuyo pake. Anthu akuyitanidwa kubwerera kwa mulungu yemwe akumukana.

III. Mutu 11:12-13:16 mwanjira ina ndi kubweredza za chigawo chotsiliza. Hoseya akuonetsa kuti chilango chawo ndi choyenera, chifukwa cha Mbiri yao yokana Mulungu kwa nthawi yaitali. Zilibe Kanthu kuti Mulungu wayetsera kwanthawi yaitali bwanji, Israyeli adapitirira kuchimwa kotero mulungu adayenera kulanga anthuwa, koma ngakhale mu nkwiyo wake sadaononge anthu onse.

IV. Kubwezeretsedwa kwenikweni kwa Israyeli mutu 14. Chisomo cha Mulungu chikuonekera pamene akulengeza kuti anthuwa azabwezeretsedwa ndipo sazalambiran so mafano. Pali kufananitsa apa pakati pa Khristu ndi Mpingo wake.

1. Monga Hoseya adakwatira Goma, koteronso Mulungu adali mwamuna wa Israyeli. Kumbukirani kuti mpingo ndi mkwatibwi wa Khristu.

2. Monga kusakhulupirika kwa Goma pamaso pa Hoseya koteronso ndi Israyeli adakhala osakhulupirika pamaso pa Mulungu. mbali yaikulu ya mpingo wa Khristu ndi osakhulupirika.

3. Monga Goma adaikidwa mu ukapolo ndi mabwenzi akewa, koteronso Israyeli adaikidwa mu ukapolo ndi maiko omwe adaika chikhulupiriro chake.

4. Monga Hoseya adakatengera mkazi wake ndikumubweretsa pa ukwati, chimodzimodzi Mulungu adzabwewdzeretsa osara a Israyeli.

5. Monga Hoseya adaombola mkazi wake ndi siliva komanso baerere, Khristu adzaombola mpingo wake (Israyeli woona) ndi mtengo wa mwazi wake.

Maulosi

1. Kuitanidwa kuchokera mu Aigoputo mutu 11:1. Pamene Israyeli anali mwana, ndinankonda, ndinaitana mwana wanga ali m'Aigoputo.

Igoputo akutanthauza ukapolo wa mu uzimu. Yesu akuombola anthu ake mu ukapolo umenewu, kotero Yesu watuluka kuchoka mu Igoputo Mateyu 2:14-15. "ndipo iye ananyamuka natenga Kamwana ndi mache usiku, nachoka kupita ku Aigoputo; nakhalabe kumeneko kufikira atamwalira Herode; kuti chichitidwe chonenedwa ndi Ambuye mwa mneneri kuti

'Ndinaitana Mwana wanga aturuke m'Aigoputo.'

2. Hoseya akunena za kukana kwa Ayuda zomwe tikuziona pamene Yerusalemu akuonongedwa mu 70 AD. Paulo mu Aroma 9:22-26 akugwiritsa Hoseya 2:23 ndi Hoseya 1:10 kulongosola kuti Ayuda ndi amitundu adzabwedzeretsedwa ku chisomo cha Mulungu kudzera mwa Khristu.

3. Kuuka kwa Khristu ndi Mpingo wake.

A. Mutu 6:2 ndiulosi onena za kuukisidwa kwa akufa kwa onse Yesu ndi akhristu ake.

B. Hoseya 13:14 ndi ulosi wakulumikidza kuwukisidwa kwa Yesu ndi anthu akufa

Kuukisidwa kwake ndi chitsimikizo chakuti ifenso tizauka kuchokera m'manda 1Akorinto 15:20

Phunziro

1. Kusankhidwa mwa chisomo. Monga Hoseya adasankha Goma mukusayenera kwake, koteronso Mulungu watisankha ife tikadali osayenera monga adalili Goma. Mulungu akuchita monga Hoseya 11:4 akunenera kuti amatiitanira ife kwa Iye yekha ndi mabande a chifundo komanso zomangira za chikondi.

2. Chifundo osati msembe ndizomwe Mulungu amazikhumba. Hoseya akuphunzitsa kuti popanda chifundo, msembe zathu ndi momwe timapembezera ndizopanda phindu Hoseya 4:1-2.

3. Utsogoleri wa anthu a Mulungu. utsogoleri wabwino ndiofunikira kwambiri, ndipo Hoseya akususana ndi utsogoleri woipa wa munthawi yake. Utsogoleri woipa umasocheretsa anthu Hoseya 4:5; 4:6; 5:1; 6:9; 10:5; 5:10; 7:3-7; 9:15.

Mathero. Bukuli ndiloonetsa chifundo. Lili ndi nkhani ya chikondi cha munthu ndi ina yokhudzana ndi Mulungu komanso Israyeli. Muli ziopsezo za zilango zoopsa ndi malongezo abwino kwambiri. Tikuona malonjezo amasiku abwino akubwera pamene tidzabwedzeretsedwe ndikukhala ndi mtendere wa muyaya. Ndi mphamvu zake za umulungu komanso chisomo chake, Ambuye mwachidziwikire adzapulumutsa anthu ake ku imfa ndi kugahena.

Yoweli

Timadziwa zochepa zokhudzana ndi Yoweri, mwachitsanzo, tsitikuziwa nthawi yomwe adalalikira uthenga wakewu. Adatumikira ku Yuda. Dzina loti Yoweri limatanthaudza kuti Yehova ndi Mulungu. uthenga wake umagwirizana ndi nthawi ina iliyonse kotero nthawi adalemba uthengawu siyofunika kwenikweni. Machenjezo adapita ku maiko onse ngakhalenso kwa ife. Yoweri akunena kuti Mulungu wabweretsa chigumula chifukwa cha machimo a anthu.

Pamene Yoweri akunena za mlili wa zombe, zikutanthaudza chipasuko chili chonse choopsa monga chivomerezi, koma munthawi iyi zinali zombe zomwe mumbiri zimaononga chakudya chakudera. Chiononge kochi chimabweretsa njala ya zaoneni kwa anthu kotero anthu amanvetsetsa chiweruzo choopsa chomwe Mulungu wachibweretsa kwa iwo.

1. Mutu 1:1-20 akulongotsola chomwe chikuchitika. Akulongosola mlili wa zombe zomwe zikuononga chili chonse chomwera; kena kalikonse kodyebwa.

A. Yoweri akunena monveka bwino kuti sapanakhale chipasuko choopsa chonga ichi vesi 2. Amafuna aliyense wa ku Yuda kudziwa za kuopsa kwake. Amafuna phunziro kuti lidzapatsidwe kumitundu yakuza nsogolo.

B. Mu vesi 15 Yoweri akunena kuti tsiku la Ambuye likubwera. Mau awa amanenedwa m'Baibulo kawirikawiri maka potsindika za chiweruzo choopsa chomwe chilinkuza. Yesaya13:6-22 akulongosola za tsiku la Ambuye ngati tsiku la tsoka.

2. Yoweri popitirira akunena za chiwembu pa mutu 2:1-11. Akupereka chinthunzi cha asilikali omwe adzaononge chilichonse chakuza. Mpiti uliwonse wa asilikali uzabwera ndi kuononga. Chiwembuchi ndi chachikuru kotero palibe akhoza kubisala.

A. Vesi 11 akunena kuti asilikali omwe azizachita zonsezi ndi asilikali a Mulungu ndipo achite chomwe Mulungu achifuna. Yoweri akutiuza kuti ili ndi tsiku la Ambuye ndipo palibe apirire tsiku limeneli.

3. Muchaputala cha 2:12-17 uthenga watsopano ukubwera kuchokera mwa Yoweri. Uku ndi kuitana anthu kuti alape. Yoweri akutiuza za kulapa koona.

A. Tikuona kuchokera mu vesi 12 ndi 13 kuti kulapa koona kumachokera mu mtima. Munthu wa nkati ndiyemwe Mulungu amamuona (1Samueli 16:7), osati zongozipanga kuti dziko lione. Kulapa koona kumachokera mumtima osati pakamwa pokha pamunthu kungonena kuti pepani.

B. Kulapa koona umatanthauzanji?

i. Kuvomereza machimo omwe tawachita. Tikuyenera kuvomeredza kuti ndi ife ochimwa.

ii. Moona tikuyenera kunva chisoni ndi machimo athu.

iii. Tikuyenera kufunafuna titasintha. Tichoke ku machimo athu ndi kutembenukira kwa Mulungu. tikuona izi mu vesi 12 ndi 13pamene Mulungu akunena kuti mutembenukire kwa Ine.

C. Pali mphoto yobwera chifukwa cha kulapa. Vesi 13 ikutiuza kuti Mulungu ndi wachifundo ndi chisomo kotero azatikhululukira ife pamene talapa. Vesi 13 ikutiuza kuti Iye azatidalitsa ife.

D. Mu vesi 15-17 tsopano akutiphunzitsa kufunika kwa ntsogoleri kutsogolera anthu ku kulapa. Ndikwabwino kuti mpingo ukhale ndi atsogoleri olapa. Tito 1:5-9 akuphunzitsa kuti akulu a mpingo akhale zitsanzo zabwino kwa anthu awo. Atsogorere mpingo kuti upite chisogolo.

4. Yoweri 2:18-32 Mulungu akulonjeza madalitso akuru kwa anthu ake pamene alapa.

A. Yoweri 2:28-32 inagwiritsidwa ntchito ndi mtumwi Petro pa Machitidwe 2:16-21mu ulaliki wake patsiku la Pentekosite. Yoweri amanenera za matsiku osiliza. Uneneriwu umanena za kubweranso kawiri kwa Yesu.

5. Mutu 3:1-21 akunenetsa kuti chiweruzo cha Mulungu chilipodi ndipo ndi cha anthu onse.

A. Vesi 1-6 akunena kuti Mulungu ali ndi dandaulo ku maiko a chikunja. Madandaulo ake ndiakuti maikowa amazunza anthu ake. Lero Mulungu amakhala okwiya pamene osapemphera akuchitira chiwembu akhristu.

B. Mulungu akuti awa ndi anthu ake chifukwa adalengedwa ndi Iye komanso Iye adawaombola.

i. Mulungu adaleng Israyeli poitana Abrahamu. Mu Genesis 15:5 Mulungu adamulonjeza Abrahamu kuti azamupatsa mbeu zochuluka ngati nyenyezi za kumwamba. Izi zimalongosola za dziko la Israyeli.

ii. Yesu adaombolanso Mpingo wake pamene adayulipirira ndi mwazi wake kotero mpingo ndi mkwatibwi wa Yesu onani Chivumbulutso 19:7

C. Mu vesi 7-13, Mulungu akuchenjeza maiko achikunja amene achitira nkhaza anthu ake kukonzekera kuchita nkhondo ndi Iye.

D. Mu vesi 14 ndi 15 mulungu akulengeza kuti posachedwa azaganizira tsoka la muyaya la anthu.

E. Mulungu akulonjeza pa vesi 16-21 kuti adzakhala pothawirapo pa anthu ake kwa muyaya. Anthu a Mulungu sazalangidwa mpaka muyaya, chifukwa cha zomwe Yesu adachita kwa ife pamtanda. Tidzakhala kumwamba ndi Yesu mpaka muyaya.

Amosi

Tsopano tiona buku la Amosi. Tikuona mu Amosi 1:1kuti adali mbusa. Iyi ndi ntchito ya munthu wamba, kotero tikuziwa kuti motsiyana ndi Yesaya iyeyu adali osaphunzira komanso wosauka. Adali m'badwa ya ku Yuda koma pa mutu 7:15 akunena kuti adatumizidwa ku ufumu wa kumpoto kwa Israyeli. Vesi 1 ikunenanso za mafumu onse a Yuda ndi Israyeli, kotero tikuziwa kuti adakhalako nthawi yomwe chuma chidali chikupita patsogolo; izi zidali zaka 30 a Asuri asanabwere kuzalanda ufumu wa kumpoto. Monga zimachitika nthawi zambiri, anthu akakhala pachuma nthawi zambiri amataya Mulungu. adali ochimwa komanso osamvera Mulungu.

1. Mu Chaputala 1:2 Amose akuuza anthu kuti anvetsere chifukwa Mulungu ali ndi chinthu chofunikira kuti alankhule nawo. Mkango akutanthauza kuyankhula kwa Mulungu ndi kubangula, chifukwa ali ndi uthenga womwe wabweretsa chiopsezo kwa anthu. "Podyetsa abusa padzachita chisoni, ndi mutu wa Karimeli udzauma", kukonzekeretsa anthu kuti nthawi yolimba ili kubwera. Phiri la Karimeli lidali nthawi zambiri linali la chinyontho mudera louma la ku Israyeli, koma Mulungu akulonjeza chiweruzo kwa Israyeli, chifukwa cha machimo awo pamene akuwuza anthuwa, kuti malo ambiri muzakhala mouma. Kotero akulosera chilala.

2. Mu chaputala 1-2:16 tikuona Amosi ku ufumu wa ku Israyeli, akulalika ulaliki okhudzana ndi momwe Mulungu adzabweretsere chiweruzo kwa maiko chifukwa cha machimo awo. Mutu 1:3 akunena kuti chifukwa cha zolakwa zitatu kapena zinayi, sadzabwedza kulanga kwake. Iyi ndi njila yoonetsa kuti tchimo lomwe lalembedwa la mzindawu silokhali lomwe anthuwa adachita. Adzalangidwa chifukwa amakhala akuchimwa kawirikawiri.

A. Mizinda yoyamba yomwe Amosi (mutu 1:3-10) waiyika pa mndandanda kuti alangidwe onsewa ndi adani a Israyeli. Chilango kwa adani amenewa ndi chimwemwe kwa Ayuda; mizinda imeneyi ndingati Damasiko, Filisiti ndi Turo.

B. Mizinda ina yomwe yaikidwa pa mndandanda kuti ilangidwe ndi; Edomu, Amani, ndi Moabu omwe ali abale a Ayuda kuchokera m'magazi. Anthu a ku Israyeli siokondwa ndi chilango chawo, koma ndizovomerezekabe chifukwa Mulungu akupitiliza kulanga anthu ena osati a Israyeli okha. Tikuona izi mu chaputala 1:11-2:3.

C. Mutu 2:4-5 akutchulanso kuti dziko lina lomwe lakhuzika ndi chilango ndi Yuda. Uthengawu tsopano ukubweretsa theng'eneng'ene, chifukwa chilango ichi chikupita kwa kwa abale awo Ayuda, koma anthu a ku Israyeli akuchivomerezabe chifukwa pamapeto pazonse anthu enanso azalangidwa. Milandu yao ndiyotsiyana ndi maiko ena omwe ali kale pa mndandanda. Milandu yao ndi ya muuzimu, ndipo ndi milando yosusana ndi Mulungu.

D. Tsopano mu chaputala cha 2:6-16, Amosi akuonetsa kuti ndi munthu otsimikidzika poyankhula, chifukwa ali mu Israyeli, koma akulengedza za chilango chomwe chikubwera kwa Israyeli. Zinali zosavuta pamene amanena za anthu ena, koma apa iyeyu ndi mlendo amene akuyankhula mosusana ndi anthu a ku Israyeli, ndipo posachedwa adakhala osafunikiranso. Pali phunziro apa kuti tikuyenera kukhala okhulupirika kwa Mulungu ndi kulalikira nthawi zonse uthenga wake, palibe Kanthu kuti uthengawo ndiotchuka kapena ayi. Tifunefune kusangalatsa Mulungu, osati kusangalatsa munthu, ngakhale kuchita izi kutha kuika moyo wathu pa chiswe. Abusa ambiri amalalika zinthu zotchuka ndicholinga chofuna kutsangalatsa anthu, koma izi ndi zolakwika. Maulaliki athu cholinga chake sikusangalatsa makutu a anthu, koma tikuyenera "kuima pa zomwe mapazi awo akhazikikapo."

E. Vuto lomwe Amosi akulinena apa ndi vuto lomwe lili mumpingo lero. Ayuda amaganiza kuti popeza ndi anthu asankhidwa ndi Mulungu chilango choopsa

sichingawafikire. Inde, Amosi anaza ku dziko lawo kuwauza anthuwo kuti ndiolakwitsa. Anthu onse adzaweruzidwa ndi Mulungu, ndipo chiweruzo chilichonse chidzatengera ntchito yomwe munthu adachita osati ubale wa mbanja lake. Kukhala mumpingo, sikupulumuka ayi. Koma chani tsopano? Koma kukhala nkhristu woona ndi chipulumutso.

F. Mutu 2:4 akutiudza chifukwa chimodzi chomwe chikupangitsa kuti Ayuda alangidwe chomwe ndi kukana Malamulo a Mulungu ndikusanvera Iye. Mulungu akuchita mofana pakati pa Ayuda ndi a Israyeli chifukwa anthuwa ndi amodzi pamaso pa Mulungu.

i. Vesi 4 ikutiuza kuti tchimo lina linali lakuti anthu osankhidwa a Mulungu adapita kukatumikira milungu ina.

G. Vesi 6-8 ndi mndandanda wa mirandu yosusana ndi Israyeli. Chinthu chomwe chaperekedwa m'mavesi osatirawaakulongosola za chinyengo chotheratu deralo, kumene olemera amabera osauka kuti alemere kotheratu. Milandu yao paokhapaokha ndi iyi

1. Mulandu oyamba ndi nkhaza pa chuma. Izi zikutanthaudza kugulitsa munthu osachimwa kuti ukhale ndi golide komanso osowa kuti ugule sandasi/nkhwaila. Mulanduwu ndi onamiza anthu osauka kuchithu chomwe adayenera kulandira powasinthanisa ndi zinthu zazikuru monga siliva kapena zinthu zazing'ono monga nsapato ya nkhwaila.

2. Mulandu wachiwiri ukupedzeka pa vesi 7 omwe ukuti chilungamo cha osauka m'mabwalo a milandu chimasokonezedwa ndi anthu olemera. Makhoti adali achinyengo kwambiri.

3. Mulandu wachitatu ukupezeka pa vesi 7 omwe ukunena zakutsowa kwa chikhalidwe; makamaka chigololo.

4. Mulandu wa chinayi uli mu vesi 8 wakulanda osauka chofunda chawo. Zinthu zimenezi zikuletsedwa pa Eksodo 22:26-27.

5. Mulandu wachinayi ukupezeka kumapeto kwa vesi 8, ndi tchimo logwiritsa makhoti a chinyengo kuti atenge ndalama kwa osauka. Anthu amalipiritsidwa chindaputsa chopweteka kwambiri.

H. Mathero a ulaliki woyamba wa Amosi uli pa mutu 2:9-16.

i. Mulungu akukumbutsa anthu mu vesi 9-11 pa zonse zomwe wachit kwa iwo komanso kuti chipambano chawo chachokera m'manja mwake.

ii. Mu vesi 13-16 Amosi akunena ndi anthu kuti ochimwa onse azalangidwa komanso Mulungu sadzakondera munthu. munthu aliyense adzaweruzidwa mofana posatengera komwe akuchokera.

3. Pa Mutu 3:1-2 Amosi wayambanso ulaliki wina. Wayamba ndikunena kuti Israyeli, ndi anthu onse ali padziko lapansi akuyenera kukhala okhulupirika pamaso pa Mulungu. koma chikhalidwe cha anthu a ku ufumu wa kumpoto chidali cholakwika kwambiri kuposa anthu amitundu omwe adawazungulira. Mpingo ukuyenera kuchita zinthu zake mwa pamwamba kutsiyana ndi anthu omwe ndi osapulumutsidwa. Ndizonvetsa chisoni kuti nthawi zambiri palibe kutsiyana pakati pa anthu amumpingo ndi anthu osapemphera. Mwachitsanzo, kulekana kwa m'banja ku magulu onse awiri (pang'ono ku Amereka) zikuoneka kuti ndichimodzimodzi. Onani zomwe Mulungu adachita ndi anthu ake;

A. Mulungu adawasankha kuti akhale anthu ake opatulika. Adawasankha pakati pa anthu onse a dziko lapansi. Sadasankhe Abrahamu chifukwa kuti Abrahamu adali munthu wonvetsetsa zinthu za mu uzimu ndi chikhulupiriro kwa Mulungu ayi. Abrahamu adali wa amitundu, pamene Mulungu ankamuitana. Mulungu adasankha anthu aku Israyeli pa

chifukwa chodziwa Iye mwini. Werengani Aroma 9:11-15 kuti mutsimikidzire. Ngati muli nkhistu, ndiye kuti munasankhidwa ndi Mulungu.

B. Mulungu adatulutsa a Israyeli ku Igoputo kunyumba ya ukapolo. Aroma mutu 6 akutiudza kuti Mulungu wapulumutsa akhristu onse ku ukapolo wa tchimo. Sindife akapolo a tchimo.

C. Israyeli pachifukwa chakuti adasankhidwa ndi Mulungu pakati pa anthu onse a dziko lapansi, adali ndi udando winawake kwa Mulungu. anthu osankhidwa a Mulungu ali ndi udindo wa pamwamba wonvera ndi kutsata Mulungu kutsiyana ndi mitundu ina ya anthu a padziko lapansi. Luka 12:47-48 akutiphunzitsa kuti anthu omwe adamva zoona za Yesu Khristu ndi kumukana Iye adzalangidwa koopsa kuposa munthu yemwe sadanve chilichonse chokhudzana ndi Yesu, panthawi ya chiweruzo.

4. Amosi 3:6-8 ndi mulu wa machenjezo kwa anthu. Mulungu akuchenjeza kuti adzapereka chilango choopsa kwa anthu amene akupitiliza kusanvera Iye.

5. Mutu 3 ukuthera ndi chenjezo lochokera kwa Mulungu palibe adzabisale pa chiweruzo cha Mulungu; sipadzakhala malo obisala. Akuwaudza kuti akhale moyo onvera Mulungu ndi chiyembekezo chakuti Mulungu awachitire chifundo.

6. Mutu 4-5:15 Mulungu akuulula zomwe amalakalaka zokhudzana ndi chipembezo. (5:21-22) Amadana ndi chipembezo chonama, pamene anthu akumana ndi kuchita zinthu zomwe zili zotsangalatsa m'maso mwawo, koma osati kupembeza Mulungu mwa chindunji ndi kumukhumba Iye Yohane 4:23.

A. Akuyamba pa vesi ponena za ng'ombe za ku Basana zomwe zikutanthaudza akazi omwe akukhala mu chuma chochuluka. Izi zikuonetsa kuti sakondwera ndi achuma, osati chifukwa alemera, koma chifukwa alemera pakupondereza osauka. Sapita kukapembeza Mulungu ndi mitima yoyera.

i. Mulungu mu vesi 2-3 akulonjeza kuthesa chuma chawo pakubweretsa chiweryzo kwa iwo. Apa maka akunena za kubwera kwa a Asuri amene adzagonjetse Israyeli ndikutenga anthu ambiri kupita nawo kutali ku ukapolo.

B. Amosi akunena za chipembezo chonyenga chomwe chinkachitika malo atatu omwe adali ofunikira m'masiku oyambirira a Mbiri ya anthu osankhidwa a Mulungu. malowa ndi Beteli, ndi Giligo, omwe akutchulidwa pa 4:3 komanso Beteseba, yemwe akutchulidwa mu 5:5. Anthu adatembenuza malo amenewa kukhala opembezera mafano. Sadanvera malangizo a Mulungu a mmene angapembezere ndikutinso akuyenera kupereka msembe kukachisi kokha.

i. Pali phunziro apa mu kapembezedwe kwa akhristu. Tikuyenera kuyang'ana m'Baibulo kuti tipeze dongotsolo la momwe tingapembezere, ndikuti tisakonze zinthu zomwe tingazitsangalatsire tokha popembeza. Cholinga chathu pamene tikupembeza ndikupereka mayamiko kwa Mulungu, ndi matamando omwe Iye akumuyenera. Sitiyenera kuyika zotsangalatsa thupi lathu patsogolo pa Mulungu. Tikuyenera kubwera kwa Iye ndi mitima yonvera komanso yoyera.

C. Amosi adapitilira kuwaudza chifukwa chomwe chipembezo cha Israyeli chili chakufa.

i. Choyamba ndi mfundo yakuti chipembezo cha Israyeli chidasakanikirana ndi kuvunda kwa chikhalidwe. Adayenjezera pa chaputala 5:7, 10-13 kuzimene adanena moyambirira zokhudzana ndi chinyengo mu chaputala 1-3. Anthu adali okhutitsidwa kuchita zinyengo ndikuchitanso chipembezo panthawi zofanana.

ii. Chinthu chachiwiri chomwe chidali cholakwika pa chipembezo chao chidali chakuti samakhudzika ndi machimo awo. Amachita msembe zothokoza, komanso

chopereka cha ufulu, koma osati msembe ya machimo. Mbali imodzi ya kupembeza kwathu kukhale kuvomereza machimo athu ndikupempha Mulungu kuti atikhululukire kotero adzalandira mayamiko athu.

iii. Chinthu chachitatu chomwe chimakwiyitsa Mulungu samafuna Iye mu mapemphero mwawo. Ankapembezo ndi zolinga zawozawo. Chitsanzo ndi Amosi 4:5 amapereka msembe za ufulu kotero kuti azitamandire okha.

D. Kenanso mu 4:6-11 Mulungu adachenjeza anthu. Adachita izi kotero kuti anthu alape ndikubwerera kwa Mulungu, koma sanalabadire Mulungu.

E. Amosi akutseka gawo limeneli mu 5:14-15 pakudandaulira anthu kuti akhale ndi moyo wokondweretsa Mulungu kotero kuti Mulungu awachitire chifundo.

7. Chaputala 5 chikutseka ndi Amosi akuwaudza anthu kuti akhale otsamala ndi "Tsiku la Ambuye" lomwe limatchulidwatchulidwa m'Baibulo. Chitsanzo chikuchokera mu Yesaya 13:6 Yoweri 1:15, Malaki 4:5 akuonetsa nthawi yoopsa kwambiri pamene Mulungu akubweretsa chiweruzo chotsapiririka. Tsiku la Ambuye likulongotsoledwa mu 2 Petro 3:10 ngati tsiku la nkwiyo wa Ambuye; nthawi yowawitsa.

A. Tiyeni tione zizindikiro zitatu za "Tsiku la Ambuye."

i. Vesi 18 ikulongotsola tsikuli ngati tsiku la m'dima. Gahena imalongotsoledwa mu Mateyu 8:12 ndi Yuda 1:13 ngati malo a m'dima wa bii. Baibulo limayerekeza kuwala ndi kupezeka kwa Mulungu; onani Masalmo 104:2, Yohane 8:12 ndi Yohane 9:5. Kuwala ndi kwabwino pamene m'dima ndi woipa. "Tsiku la Ambuye" lomwe Amosi akulilongotsola ndi nthawi ya chiweruzo cholapitsa. Ndi nthawi pamene walekanitsidwa ndi Mulungu zomwe zikutanthaudza kulekanitsidwa ndi chinthu chilichonse chabwino; onani Yakobo 1:17. Izinso zikufotokozera za Gahena komwe tikalekanitsidwe ndi Mulungu kwamuyaya.

ii. Chizindikiro china ndichakuti Mulungu sathawika; sungathe kuthawa Mulungu. tikuona mu Amosi 5:19 pamene munthu amathawa mkango koma kupedzekanso kuti kutsogolo kwake kuli chimbalangondo ndi chinjoka.

iii. Chizindikiro chachitatu chomwe chikupezeka pa Amosi 5:20 ndichakuti alibe chiyembekezo munthu amene akutsutsana ndi Mulungu.

B. Amosi akutseka izi mu vesi 23-24 polemba kuti nthawi ilipobe yothawa nkwiyo wa Mulungu. pamene munthu ali ndi moyo antha kuthawa "Tsiku la Ambuye" potembenukira kwa Yesu kuti akhale Ambuye ndi Mpulumutsi wake.

C. "Tsiku la Ambuye" si tsiku loopsa kwa Akhristu chifukwa ndi tsiku lomwe akhristu adzakhale akupita kumwamba.

8. Mutu 6 ndikutupsa anthu omwe akukhutitsidwa ndi momwe zinthu zilili. Izi zidali zolakwika munthawi ya Amosi ndiponso ndi zolakwika mumpingo lero. Akhristu ambiri amaoneka kuti sazindikira kuti pali nkhondo ya muuzimu yomwe ali kuchitika. Bola ngati moyo ulibwino, amakhala okhutitsidwa, posalabadira anthu ambiri omwe awazungulira amene ali kuchionongeko ndipo amatero ponena kuti akupewa choipa. Tikuona izi ku mpingo wa ku ulaya kumene mpingo ukulephera kuchita evanjelizimu makamaka m'mamishoni akunja kwa dziko lawo. Akhristu ambiri amayetsera kuzemba choipa ndikuyetsetsa kuchithetsa monga kuthesa kutaya mimba, komanso kufalikira kwa maukwati a pakati pa anthu ofanana ziwalo. Mateyu 16:24 ndi chitsanzo chimodzi chokha mwa zina zambiri m'Baibulo zomwe zimaphunzitsa kuti ife akhristu tikhale amachawi maka potumikira Mulungu. Nthawi zambiri akhristu amalephera kuzindikira kuti chigumula chawazinga ndipo pali chiopsezo chachikuru.

9. Mutu 7:1-9 ndi 8:1-9:10 muli masomphenya asanu.

A. Maso mphenya oyamba akupezeka mu vesi 1-3 pamene Mulungu akuopseza kuti abweretsa zombe zomwe zikutanthaudza njala kwa anthuwo. Amose adapempha Mulungu kuti asalange anthuwo ndipo Mulungu sadalangedi anthuwo

B. Masomphenya achiwiri akupezeka pa vesi 4-6 ndiokhudzana ndi moto komwe kuli kuopseza za kuuma kwa derali, mwanjira ina kudzakhala chilala muderali.

C. Masomphenya achitatu ali mu vesi 7-9 ndipo akunena za Mulungu yemwe wagwira chingwe cholungamitsa chiriri. Mulungu akunena kuti akuyeza kapena kuyetsa Israyeli ndikuona ngati Israyeli akukhala moyenerera monga momwe Mulungu akuyembekedzera anthuwa kukhalira. Tikuziwa kuti Israyeli saakhala monga momwe Mulungu amayembekezera, kotero mu vesi 9 Mulungu akuopseza kuti awononga Israyeli. Tidzapewa chionongeko chimenechi ngati tikhulupirira mwa Ambuye Yesu monga Machitidwe 16:31 akunenera komanso monga Mchitidwe 2:38 akunenera kuti lapa ndi kubatizidwa.

i. Chingwe cholungamitsa chiriri kwa akhristu ndi Baibulo lomwe limatipatsa mulingo wa momwe tingakhalire.

D. Mathero onse a mutu 7 chiwembu cha Amaziya kwa Amosi, mkuru wa chipembezo amene adakamunenera Amosi mlandu kwa mfumu. Amaziya adamulamula Amosi kuti asiye kulalika ndikubwerera kwawo ku Yuda. Amosi adanvera Mulungu ndikuuza Amaziya mu vesi 17 kuti Amaziya ndi dziko lonse adzathedwa psiti. Tikuyenera nthawi zonse kulalika mopanda mantha komanso kulalika choona kuchokera m'Baibulo.

E. Masomphenya achinayi akupezeka pa mutu 8 ndipo koyamba mu vesi 1-2. Akunena za ntanga wa zipatso za m'malimwe omwe ukuoneka kuti ndiwabwino. Komabe zipatsozo zikutcholedwa, ndipo zili kumapeto koti zithe. Sipadzakhalanso kukolola kopitirira; sipadzakhalanso madalitso opitilira kuchokera kwa Mulungu.

i. Kumapeto kwa chaputala chonsechi kuyambira pa vesi 3 tikuona mndandanda wa mavuto a Israyeli. Vesi 8-11 akunena za momwe dzikoli lizavutikire ndi njira ya uzimu. Mulungu adzawachokera anthuwo. Tikuona izi m'malo ambiri momwe chikhristu chidali chotentha, koma pano m'malo m'menemo ndi mwachikunja. Tikuziona izi kumalo ngati ku Ulaya komanso ku Canada/united States.

F. Masomphenya osiliza akupezeka mu chaputala 9:1-10 akunena za mathero a Israyeli. Mulungu akulengeza kutha kwa pangano lapadera la ubwenzi wake ndi Israyeli.

i. Vesi 1-6 akunena za kutha kwa Israyeli zomwe zidachitika patangotha zaka 50 pambuyo pa Amosi atanenera ulosiwu. Tikuwerenga m'mavesi amenewa kuti ndizosatheka kuzemba chiweruzo cha Mulungu.

ii. Gawo lachiwiri la ulosi umenewu likupezeka pa vesi 7-10 lomwe likunena za kuthedwa kwa mpingo. Vesi 7 akunena kuti Mulungunso sakuona anthu awa ngati opatulika ayi. Ndiofanana ndi anthu a ku Kusi. Anthu mu vesi 10 akunena momwe akuganizira poziyetsa kuti ndiopatulika ndikuganizira kuti Mulungu azawateteza ku chionongeko.

iii. mu vesi 8 ndi vesi 9 Amosi akuuza anthu kuti pamene anthu ambiri a ku Israyeli adzaonongedwa, koma Mulungu sadzaononga ochepa oopa Iye. Nthawi zonse azasunga anthu ake okhulupirika.

10. Mavesi osiliza a Amosi kuchokera vesi 11-15 akulonjeza kuti Mulungu azabweretsa nthawi yopatulika kwa ana a Israyeli. Bukuli likusiliza ndi malonjezo a tsogolo la dalitso kwa Israyeli. Tikuona zambiri zokhudzana ndi ganizo limeneli mu Aroma 11. Pali zinthu

zochepa zoti tichitire ndemanga, pa nthawi ya dalitso yomwe ikubwera ku tsogolo kwa Israyeli.

A. Padzakhala dalitso kwa a Israyeli pawokha. Vesi 11-12.

B. padzakhala nthawi ya madalitso a chuma. Vesi 12-13.

C. Madalitsowa adzakhala okhadzikika. Vesi 15.

Obadiya

Tsitikudziwa kuti Obadiya adali ndani, kapenanso nthawi yomwe adalemba bukuli. Ngakhale lili buku laling'ono mu Chipangano chonse Chakale, koma lili ndi phunziro kwa ife. Mulungu ndiolekerera kwambiri, koma kulekerera kumeneku kuli ndi malire, ndipo pamene sangathe kupiriranso, chilango chake chimakhala chopweteka kwambiri. Izi zidali chomwechi mu Chipangano Chakale ngakhalenso m'masiku athu ano.

Obadiya ndi mneneri yemwe amayang'ana kwambiri za kugwa kwa Edomu, dziko lomwe lidali m'dani wa nthawi ya itali kwa Israyeli komanso woyandikana naye. M'bale wake wa Yakobo, Esau ndiyemwe adapedza mzinda umenewu. Kwa nthawi yayitali mu Mbiri, Edomu wakhala ali m'dani wa Israyeli. Edomu amaziona yekha kuti ndi otetezeka mu dziko lake komwe kudali ku m'mawa kwa msinje wa Yordani. Dzikoli lidali m'madera a kuphiri komwe kunali kovuta kuti adani awo awagonjese. Lero dera limeneri lili m'manja mwa anthu a dziko la chisilamu la ku Yordani.

Zikuoneka kuti, nthawi zambiri Edomu adachita mosusana ndi Israyeli. Mwachitsanzo, Mose, adapempha mfumu ya ku Edomu kutenga anthu aku Israyeli kuti aduse mudzikoli popita kudziko la malonjezano la Kanani. Nkhaniyi monga ikunenera mbuku la Numeri 20:14-21, akunena za momwe Edomu adaopsera Israyeli kuti akangolowa m''dziko lawo amutha ndi nkhondo. Kenako mu Numeri 24 Balamu adalotsera kugonjesedwa kwa Edomu ndi a Israyeli.

Mutu 1:1-9 Obadiya adalotsera kuonongedwa kwa Edomu. Izi zikuchitika posayang'anira chitetezo chomwe Edomu adali nacho chifukwa chakuti amakhala kuphiri, adali wachuma komanso adali ndi asilikali amphamvu.

Vesi 10-14 akuonetsa chifukwa chomwe chikupangitsa kuti Edomu alangidwe chomwe ndi kuchitira a Israyeli choipa. Pamene a Israyeli adagonjesedwa, Edomu pamodzi ndi adani a Israyeli anapanga m'gwirizano osalaza Israyeli. Monga vesi 10 ikunenera nkhazi imene idachita a Edomu adachita kwa mchimwene wake Israyeli.

Gawo lotsiliza la Obadiya likuyamba mu vesi 15 lomwe likubweretsa chiweruzo cha Mulungu. vesi 15 ikutiuza ife kuti tsiku la Ambuye lili pafupi kuza m'maiko onse. Tsiku la Chiweruzoli lizakhala zotsatira za kutha kwa Edomu, kutha kukhala ngati kudalibenso Edomu. Tsiku la chiweruzo likutanthauza kuomboledwa kwa Israyeli.

Gawo losiliza la Obadiya lomwe likuyambira mu vesi 17, likunena za kubwedzeretsedwa kwa Israyeli. Israyeli adzalangidwa ndi Mulungu koma kwa kanthawi kochepa. Chilango cha Edomu chizakhala chokhazikika/chotsatha pamene Israyeli akulonjedwa tsogolo la ulemerero.

Pali zinthu zitatu zomwe vesi 17 ikutiphunzitsa ife zokhudzana ndi lonjezo la Mulungu lonena za tsogolo la dalitso. Malonjezowa ndi malonjezonso a akhristu. Malonjezowa ndi;

1. Tsiku la Ambuye ndi tsiku lakuomboledwa kwa anthu a Mulungu. Ndi tsiku lomwe ife akhristu tidzaomboledwe ku ukapolo wa tchimo lathu.

2. Vesi 17 likunena zakukhala oyera. Kwa akhristu izi zimatanthaudza kuti Mulungu adzatipanga ife kukhala oyera. Tizapangidwa kukhala oyera mwapang'onopang'ono ndipo tidzakhala oyera kwanthunthu tikazamwalira.

3. Vesi 17 ikunena momwe a Israyeli azakhalilenso m'dziko lawo, ndipo ikunena kwa akhristu kuti Mulungu azapereka zosowa zathu.

Yesaya 63:1-4 ndi uneneri okhudzana ndi chiweruzo chosiliza akazabwera Khristu kachiwiri. Tikupasidwa chithunzi cha munthu wa ku Edomu amene wakhala akupha adani ake. Munthu yemwe akuchokera ku Edomuyu ndi Yesu amene akubwerera ku Yerusalemu atatha kugonjesa adani ake onse makamaka a Edomu mwamphamvu. Pamene akuBabulo adagonjesa Yerusalemu ndikutenga anthu kupita nawo ku ukapolo zidaonetsa kuti Israyeli adathedwa monga ngati dziko. Koma nthawi yomweyo, zidaonetsa ngati Edomu lizakhala dziko lanthawi yaitalikomanso lotetezeka m'dziko lomwe ali kukhala. Komabe Obadiya adalotsera za kuthedwa kwa Edomu ndi kubwedzeretsedwa kwa Israyeli.

Apa mu buku la Yesaya tikuona kuti Yesu wagonjesa adani ake onse padziko lapansi makamaka pamene waweruza Edomu. Yesu akubwerera kwa anthu ake a Israyeli pamene wamaliza kuweruza dziko lapansi.

Edomu adazimirira angakhale Yesu asanabwere pamene Israyeli alikobe lero wathanzi. Edomu kubelinso.

Yona

Mneneri wosiyana mtundu, Yona adatumidwa kukapulumutsa anthu omwe si a Israyeli, koma kukapulumutsa anthu omwe adali adani awo aku Nenevi likuru la dziko la a Asuri. Nkhaniyi imatitsimikidzira kuti Mulungu amatsamalira anthu onse osati Ayuda okha. Uyu ndi mneneri m'modzi yekha yemwe amadziwika ku Ulaya amene nkhani yake imadziwika bwino ndi akhristu komanso ndi ana omwe. Ndinkhani yokhweka komanso yosangalatsa. Yona monga momwe mwawerengera ndi munthu ovuta kwambiri. Tiyeni tione mwachidule bukuli. Bukuli lili ndi machaputala anayi. Tikamawerenga bukuli limatiudza kuti Yona anali munthu ovuta. Sadanvere Mulungu ndipo adapsa mtima Yona chifukwa Mulungu sadaphe anthu aku ku Ninevi.

Tiyeni tione nkhaniyi. Yona adatumidwa ndi Mulungu kupita ku Ninevi kuti akachenjeze anthu kuti alape ndipo akalephera adzalandira chilango. Yona sadanvere Mulungu, ndipo adalowa mu chombo chopita kwina, kotero chidwi chopita ku Ninevi chidachoka. Mulungu adatumiza namondwe woopsa ndipo chombo chidayamba kumira ndipo anthu anthu mu chombocho padaponyera Yona m'madzi, ndipo nthawi yomweyo namondwe adaleka.

Kenako nsomba inabwera ndikumiza Yona. Atakhala m'mimba mwa nsombayi kwa masiku atatu zidapangitsa Yona kulapa, kotero adavowereza kupita ku Ninevi. Kotero adapita ku Ninevi kumene anakalalika ulaliki oyitana anthu kuti alape. Ndipo nkhaniyi ikutha Yona ali chikwiire chifukwa cha kulapa kwa anthu a ku Nineve, zinthu zomwe Yona sadaziyembekezere.

Tiyeni tione chomwe tingaphunzire pamene tikuzukuta machaputala anayiwa.

1. Mulungu akuphunzitsa anthu ake ali ndi udindo okalalika uthenga wake wa chipulumutso kwa anthu onse. Ili lidali vuto lalikuru kwambiri kwa Ayuda munthawi ya Yesu onani Luka 4:26-29. Pamene Yesu amanena za dalitso la Mulungu kuti lilinso kwa anthu amitundu Ayuda anapsa nazo mtima, ndipo anafunafuna kupha Yesu.

2. Tikuona kuti mulungu amalemekeza kulapa machimo kwa anthu.

Bukuli lili ndi zigawo zinayi.

1. Yona afunafuna njira yakeyake 1:1-16. Mulungu adamulamula kuti apite ku Ninevi, m'malo mwake Yona adalowa muchombo chopita ku m'mawa. Powona kusanvera kwakeku Mulungu adautsa namondwe woopsa, ndipo Yona adaponyedwa m'nyanja namira.

2. Mutu 1:17-2:10 Mulungu akukulitsa chisomo kwa Yona potumidza nsomba kuti imumeze ndikuteteza moyo wa Yona kotero kuti Yona apite kukagwira ntchito ya Ambuye. Yona adapemphera ndipo nsombayo inakamulavula Yona kumtunda. Yona anatha masiku atatu ali m'mimba mwa nsomba; inalitu nthawi ya masautso; kunvera Mulungu ndi chitsankho chabwino choti tipange. Yohane 1:17 ndi Mateyu 12:40 Yesu akunena za masiku atatu m'mimba mwa nsomba poyerekeza ndi matsiku atatu omwe Iye adzakhale ali m'manda.

3. Yona analalika ku Ninevi 3:1-10. Uthenga wake ndi wachidule ndi wachindunji. "Kwasala masiku makumi anayi ndipo Ninevi adzaonongedwa." Mu kudabwitsidwa kwa Yona, anthu onse kuphatikizirapo amfumu adakhulupirira uthengawu ndipo analapa ndipo Mulungu adawakhululukira. Phunziro apa ndilakuti sikuchuluka kwa mawu komwe kumapangitsa ulaliki kukhala opindulitsa koma m'malo mwake imakhala mphamvu ya Mulungu yomwe imapangitsa mau olalikidwawo kukhala ndi mphamvu yopulumutsa.

4. Mutu 4:1-11, Yona adakwiya chifukwa Mulungu adawakomera mtima anthu a ku Ninevi nawapulumutsa. Yona adakwiya kufika pa mulingo ongolakalaka imfa panthawi yoyamba chifukwa Mulungu adakhululukira anthuwo, kenako anapsa mtimanso chifukwa Mulungu adaumitsa mtengo omwe udali nthuzi kwa Yona. Mu vesi 10-11 Mulungu adalankhula ndi iye pakhalidwe lake loika moyo wake mtengo ndikusalabadira miyoyo ya anthu 120,000 ndi ana okhala mu Ninevi omwe adapulumutsidwa. Mulungu apa akuonetsa kukhudzika ndikuchitira chifundo anthu omwe alapa tchimo. Mulungu pogwiritsa ntchito Yona zikuonetsa kuti sinthawi zonse zomwe Mulungu amagwiritsa ntchito anthu abwino mu ntchito zake.

Mika

1. Mika ndi Yesaya amanenera nthawi yofanana, ndipo nthawi zambiri uthenga wao umaoneka ofana. Yerekezani Mika 4:1 ndi Yesaya 2:3. Mika adali mneneri yemwe amakhala ku Yuda. Tingoona zochepa za ziphunzitso zake chifukwa cha nthawi komanso kufanana kwa uneneri wake ndi aneneri ena.

2. Kwambiri, uthenga wake ndiwakuti ngakhale Mulungu amadana ndi tchimo la anthu ake kopabe Iye amakonda anthuwo. Iye ndi Mulungu amadana ndi njira yomwe olemera amachita pomabera anthu osauka, onani Mika 3:1-3. Mukuganiza kuti mulungu akumuona bwanji Africa nthawi ino? Mika mu 7:3 akutchulanso tchimo la chinyengo. Uthenga wa Mika ndiwakuti anthu akuchimwirachimwirabe ndipo tchimoli lazindikiridwa, ndipo anthu akulonjezedwa kuti adzalangidwa ngati apitiliza kuchimwa. Uthengawu ikutseka ndi lonjezo la sogolo la chipulumutso.

3. Tikuona mu Yesaya ndi m'buku la Mika kuti aneneriwa amakonda anthu awo ngati Mulungu posawerengera machimo awo. Tkuona chikondi cholingana cha Paulo ndi anthu ake, onani Aroma 9:3. Chizindikiro cha Mbusa woopa Mulungu ndichakuti amalalikira Baibulo lonse kuphatikizapo mauthenga ovuta kwambiri. Amapereka uphungu molingana ndi Baibulo ngakhale anthu atakhala kuti sakufuna malangizo otere. Amakondanso anthu ake ndikuvulaza ena ndi mau iwo amene nthawi zonse iye amakhala akuwalilira.

4. Pali mavesi awiri mu bukuli omwe ali ngodya omwe tikufuna kuti tiwatchule. Mika 6:8 akuti "Iye anakuuza, munthuwe, chomwe chiri chokoma; ndipo Yehova afunanji nawe

koma kuti uchite cholungama, ndikukonda chifundo ndikuyenda modzichepetsa ndi Mulungu wako?" tikuona mu vesi imeneyi chomwe Mulungu akufuna kwa munthu aliyense.

Mika 7:18 akuti "Ndani Mulungu ofanana ndi Inu, wakukhululukira mphulupulu, wakupitirira zolakwa za otsala cholowa chache?." Apa Mika akutionetsa ife mfundo yakuti Mulungu mwini tsiku lina adzakhululukira machimo athu.

5. Mika 5:2-4 akunena zokhudzana ndi kubwera kwa Mesiya, ndipo kuti adzabadwira ku mzinda wa Yerusalemu mu dera la Efrata. Tikudziwa kuti izi zidachitikadi.

Nahumu

Nahumu ndi mneneri wachiwiri kwa aneneri omwe amanenera zokhudzana ndi Ninevi likuru la a Asuri. Yona anali mneneri woyamba ku Ninevi ndipo uthenga wake unali woitanira anthu ku kulapa kuti apewe chionongeko. Anthuwo analapa ndipo Mulungu anawapulumutsa. Ndipo panthawi ino, mneneriyu saitaniranso anthu ku kulapa, koma m'malo mwake akuuza anthu kuti Mulungu akubweretsa chiweruzo choopsa ku mzindawu. Zikuonetsa kuti kulapa komwe kudachitaka potsatira uthenga wa Yonasi kunatenge nthawi yaitali, ndipo anthu potsakhalitsa adabwereranso ku moyo wawo wakale.

Njira zawo zakale zidali zoipa; Ninevi amadedwa kwambiri chifukwa adali anthu ankhaza. Mzindawu udapezedwa masiku oyambirira; Genesis 10 akunena kuti Nimrodi ndiyemwe anapeza mzinda wa Ninevi. Anali anthu amphamvu amene analamulira ufumu waukuru kwa nthawi yaitali. Ninevi amakhulupiriridwa kuti amazunza anthu, mwachitsanzo Mbiri yao imanena kuti amachitsa munthu chikopa chake akadali ndi moyo.

Ulosi wa Nahumu ukutiuza kuti pamene Mulungu amagwira ntchito ndi anthu ake osankhidwa, Iye ndi Mulungu wa anthu onse ndipo anthu onse adzayankha kwa Iye ndipo adzawaweruza. Phunziro lina apa ndilakuti, ngakhale Mulungu ali Mulungu wachikondi, Iyenso ndi Mulungu wachilungamo, ndipo chiweruzo chache ndichoopsa kwambiri.

Chaputala choyamba chikunena za mphamvu ya Ambuye, ndi chilango choopsa chomwe chikubwera kwa adani ake. Tikuonanso kuti Mulungu, ali ndi ubwino kwa anthu ake, omwe akukhulupirira mwa Iye. Vesi 8-9 akunena monveka bwino kuti Mulungu adzatha psiti adani ake onse. Anthu amangofuna kunva za ubwino ndi chifundo cha Mulungu, koma tikyenera tidziwenso kuti chiweruzo cha adani ake ndichoopsa kwambiri-onani Yesaya 63:1-6 kuti muone chitsanzo china cha zinthu izi.

Chaputala 1:15-2:2 ndi uthenga wa Yuda kuti akuyenera kunvera Mulungu ndipo Mulungu pamapeto pake adzawabwedzeretsa Yuda. Chaputala cha 2 ndi 3 akunena mwatchutchutchu za chionongeko cha Ninevi.

Zomwe tikuphunzira kuchokera m'bukuli:

1. Chaputala 1:2 kachiwiri chikutiphunzitsa phunziro la Ekisodo 20:5-6 kuti Mulungu wathu ndi wansanje ndipo tikuyenera kumulambira iye yekha basi.

2. Tikudziwa kuti Nahumu anali mneneri woona wa Mulungu chifukwa Mbiri imanena za kuonongeka kotheratu kwa Ninevi, ndipo mpaka lero Ninevi kulibe.

3. Mulungu wapereka chenjezo lonveka bwino la kuonongeka kotheratu kwa anthu onse omwe amamuukira Iye komanso iwo amene samulambira Iye. Chenjezoli lilipo mpaka lero monga momwe linalili munthawi ya Nahumu. Imfa ina yomwe ili yamuyaya ku Gahena ikulonjezedwa kwa Adani a Mulungu onani Chivumbulutso 21:8.

Habakuku

Sitidziwa zambiri zokhudzana ndi Habakuku, koma anali mneneri kwa Ayuda patangotsala kanthawi kochepa kuti Yuda agonjesedwe ndi Babulo. Itha kukhala nthawi pamene Yosiya mfumu yoopa Mulungu inangochoka kumene pampando wa chifumu. Yuda adachoka pamaso pa Mulungu, kotero adayamba kukhala mwachilendo pamaso pa Mulungu. Habakuku adali m'modzi mwa aneneri amene Mulungu adawatumiza kuti ayitane anthu ake ku kulapa machimo awo ndikubwerera kwa Iye.

I. Mutu 1:1-11 pali kuyankhulana koyamba ndi Mulungu. inali nthawi ya uchimo wa zaoneni ku Yuda. Anthu amapembeza mafano komanso anali ochimwa chifukwa cha kupanda chikhalidwe. Atsogoleri awo anali achinyengo komanso ukanirira mu uchimo.

A. Tikudziwa kuchokera mu vesi 2 kuti Habakuku anakhala akupemphera kwa nthawi ndithu kupempherera machimo a anthu, ndipo amaona ngati Mulungu sakumunva. Adaona kuti anthuwo ataya Mulungu kotheratu, ndikutembenukira ku mafano. Ngakhale atsogoleri anali achinyengo. Habakuku, vesi 3 samanvetsa chifukwa chomwe Mulungu amalorera tchimo kuti lizikulirakulirabe. Habakuku samanvetsetsa kukhala chete kwa Mulungu. Mulungu anayankha pa vesi 6 kuti adzalanga anthu ndipo adzagwiritsa ntchito akasidi/ dzina lina la anthu a ku Babulo, kuti awalange.

2. Kuyankhulana ka chiwiri ndi Mulungu kukuchitika pa chaputala 1:11-2:20. Habakuku mu vesi 13 akunena kuti Mulungu sazalekerera choipa, kotero Habakuku akufuna kudziwa mmene Mulungu adzagwiritsire ntchito anthu oipa kulanga anthu ake.

A. Mutu 2:1-4 ikunena kuti anthu a Mulungu, akuyenera kukhala odekha kufikira pomwe Mulungu adzakhale okonzeka kuti achite chomwe chinkomera. Tikuyenera kukhala mwa chikhulupiriro ndi kudalira Mulungu kuti achite zomwe zili zabwino panthawi yake.

B. Mulungu akupitirira kunena kuti akudziwa bwino za kuipa kwa Babulo, ndipo kuti chilungamo chothamanga chikubwera ndipo anthu a ku Babulo adzalangidwa molapitsa.

C. Vesi 14 ikulonjeza kuti ndondomekonso ina ya dziko lapansi ikubwera ndipo moyo udzakhala otsiyana ndi lero.

D. Gawo ili likusekedwa mu vesi 20 ndi mfundo yakuti Mulungu akuyendetsa chilichonse, ndipo dziko lonse lidzaima pamaso pake pamene adzakhale akuliweruza.

3. Mutu 3 ndi pemphero la matamando. Habakuku akudzichepetsa yekha pamaso pa Mulungu ndikuyamika Ambuye chifukwa cha chiyero chake, chilungamo chake ndi ungwiro wake. Akuyamika Mulungu chifukwa cha ulamuliro wake pa zinthu zonse. Mu vesi 2 Habakuku akuuza Mulungu kuti akumbukire kuchita chifundo panthawi imene akubweretsa chiweruzo choopsa. Akutseka buku lake akulemba kuti akutsangalala mwa Mulungu amene ali chipulumutso ndi chilimbikitso chake.

4. Zomwe tikuphunzira munkhaniyi

A. Anthu safuna kukhlupirira chiweruzo cha Mulungu pambali pa machenjezo ake. Paulo mu Machitidwe 13:41, adagwiritsa Habakuku 1:5 kuti achenjeze Ayuda. Ngakhale anthu akuchenjezedwa kawirikawiri, zokhudzana ndi chiweruzo cha Mulungu, komabe akukanika kukhulupirira. Anthu ambiri amva uthenga wabwino komabe kupitiriza kukana kukhulupirira mwa Yesu Khristu pa chipulumutso chawo.

B. Habakuku akunena zakukhala mu chikhulupiriro mu chaputala 2:4. Anthu a Mulungu ali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu. amakhulupirira Mulungu munyengo ya kukondwa ndi kulira. Muyerekeze ndimomwe Yesu adakhulupirira Mulungu ngakhale munyengo yake ya nsautso m'munda wa Gesemane (Mateyu 26:39).

5. Mathero. Zikuoneka kuti oipa amachita bwino, koma izi zimangochitika kwa kanthawi kochepa. Komabe pamapeto pake amakumana ndi chiweruzo cha Mulungu. ili ndi

chenjezo kwa anthu osakhulupirira amene akutsangalala ndi moyo wao ndikutsatchera khutu ku zinthu zokhudzana ndi Mulungu. Chiweruzo chikubwera kwa munthu wina aliyense. Munthu amene Sali nkhristu adzaweruzidwa ngati ochimwa chifukwa cha machimo awo ndipo adzaponyedwa ku Gahena.

Zefaniya

Ili ndi limodzi mwa mabuku osawerengedwa kwambiri m'Baibulo. izi ndizonvetsa chisoni chifukwa uthenga wa Zefaniya ndiofunikira masiku ano monga momwe unalili panthawi yomwe umaperekedwa zaka 2500 zapitazo. Mavesi ochepa a kumapeto ndi mavesi otonthoza makamaka chaputala 3:17. Tikudziwa kuti Zefaniya anatura uthenga wakewu munthawi ya mfumu Yosiya, yomwe idali pafupi ndi kutha kwa ufumu wa Yuda. Patangotsala pang'ono kuti Yuda agonjesedwe ndi Babulo. Nthawiyi ndikuti ufumu wa kumpoto utagonjetsedwa kale ndi a Asuri.

Chigawo choyamba cha Zefaniya mutu 1:1-2:3 akukamba zokhudzana ndi kubwera kwa tsiku la Ambuye zomwe zikutanthaudza kuti uthenga wa bukuli ndi chiweruzo choopsa. Zikuchita kuoneka ngati Zefaniya buku lakeli walemba chidule cha uthenga wa mneneri wina, pamene amalemba uthenga wolonjeza chipasuko chachikuru, onani vesi 1:1-4. Kalembedwe koteroka kumatchedwa kukudza, zomwe zikutanthaudza kulemba mochemerera china chake monga chionongeko chomwe chikutchulidwa m'mavesiwa. Mulungu sizoona kuti akufuna aphe wina aliyense, monga vesi 2 ikunenera, Mulungu ali wokwiya ndipo chipasuko chidzakhala choopsa kwambiri ndipo anthu onse adzaopa.

Mulungu ndiokwiya chifukwa cha machimo ambiri kwa anthu onse; onse ndi ochimwa osati owerengeka mwa iwo koma onse ndipo uchimo wao uli pena pali ponse mwachitsanzo;

1. Muchipembezo. Vesi 4-6 akunena za machimo a chipembezo pakati pa amsembe ndi anthu. Anthuwo ndioyipitsidwa ndi mafano, ndikugwa kuchoka muchipembezo choona. Kwambiri anthuwa amakonda ndalama kwambiri kupotsa Mulungu, komanso amakonda zinthu komanso anthu anzao kupotsa Mulungu. amakonda machimo awo kupotsa Mulungu, komanso udindo wao kwa anthu ena kuposa Mulungu. Monga Mateyu 22:37 akulamulira, samalabadira lamulo limeneri lomwe likuti "uzikonda Ambuye Mulungu wako ndi mtima wako wonse, ndi moyo wako wonse, komanso ndi mzeru zako zonse."

2. Chikhalidwe chawo. Vesi 8-9 anthu mainvetsetsa motsiyana. Ine maganizo anga ndi awa. Chifukwa china chomwe Mulungu anakwiya ndi anthuwo chikupezeka pa vesi 8 chomwe chikunena zokhudzana ndi atsogoleri a anthu omwe amatsogolera anthuwa kunyoza Mulungu. umboni wa mavalidwe a chilendo zikutanthaudza kuti anthuwa amafuna kutengera chilichonse chomwe maiko ena amachita malo mokhala motsiyana ndi iwo eni ake komanso kukhutitsidwa ndi chikhalidwe chawo. Anaiwala kuti Mulungu anasankha anthu ake kuti akhale osiyana ndi ena (Deuteronomo 7:6).

A. Mbali yoyamba ya vesi 9 pamene vesiyi ikuti Ndipo tsiku ilo ndidzalanga olumpha chiundo, zikutanthaudza anthu omwe akutsatira nchitidwe wolambira mulungu wonama wotchedwa Dagoni, onani 1 Samueli 5:5. Mbali yachiwiri ya vesi 9 ikutanthaudza anthu amene ali ndi chidwi chochita chipembezo cha cha mulungu wonama Dagoni ndipo sanvera Malamulo a Mulungu. kusanvera uku kukukhudzana ndi kusanvera Malamulo a Mulungu mu chilungamo ndi ulemu.

3. Zachuma. Dera lina lomwe likupangitsa Mulungu kukhala okwiya likupezeka mu vesi 1:11 ndipo ukunena za chinyengo komwe ogulitsa amanamiza anthu m'malo ogulitsilamo malonda.

4. Kulekerera. Mulungu anakwiya chifukwa vesi 12 ikunena kuti anthu amakhulupirira kuti Mulungu sachita kantha, ndipo anthu atha kuchita chilichonse chomwe chili cowakondweretsa khaya ndi chabwino kapena ndi choipa. Koma molakwika amanva kuti Mulungu sadzawalanga chifukwa cha khalidwe lawo loipa.

Kenako Zefaniya akutiudza kuti kuchitapo Kanthu kwa Mulungu chifukwa cha machimo a anthu ndi kubweretsa chiweruzo choopsa kwa anthu. Vesi 14 kachiwiri ikunena za chiwerudzo choopsa cha pa tsiku la Ambuye. Mulungu wakhala akupitirira kulonjeza kuchokera mu chaputala cha 1 chiweruzo chotsalapika kwa anthu chifukwa cha machimo awo.

Gawo loyamba lokhudzana ndi chiweruzo likusekedwa pa chaputala cha 2:1-3 ndi Zefaniya akuitana anthu kuti alape ndikunvera Mulungu ngati akufuna kukhala ndi chiyembekezo komanso kupulumuka ku chiweruzo cha Mulungu chowe chili pafupi.

1. Dziwani kuti Mulungu ndiokwiya kwambiri akunena mu chaputala cha 2:3 kuti mwina anthu azapulumuka mu chiweruzo chake. Sakulonjeza kuti adzapulumutsa iwo monga momwe anachitira zaka 100 zapitazo munthawi ya Amosi. Anali wokwiya chifukwa cha tchimo la anthu munthawi ya Amosi komabe adawapatsa lonjezo, mu Amosi 5:6, lakuti adzapulumutsa anthu omwe alapa ku chiweruzo. Kulekerera kwa Mulungu kuli ndi malirekoteronso sitifunika kupyora malirewa.

Gawo lotsatira la Zefaniya likupezeka mu chaputala 2:4-3:8 pamene akukulitsa chiweruzo kupita kwa anthu onse a padziko lapansi kuphatikidzapo Ayuda. Mulungu ndi Mulungu wa anthu onse ndipo monga tionera vesi 8 kuti anthu onse adzalangidwa. Phunziro matsiku ano ndilakuti munthu wina aliyense akaweruzidwa malingana ndi mmene ulili ubale wake ndi Yesu.

Gawo losiliza la Zefaniya likupezeka mu chaputala 3:9-20 ndipo ndi uthenga wa chilimbikitso; uthenga wakubwedzeretsa. Tikmaona aneneri ang'onoang'ono titha kuona kutsalimbikitsika chifukwa amakamba kwambiri za chiweruzo choopsa. Komabe, ziweruzozi, simau osiliza a Mulungu. palibe Kanthu kuti chiweruzo ndichokhwima bwanji, Mulungu pamapeto pake akupereka mau a chiyembekezo kwa iwo amene alapa. Satana adzaweruzidwa ndipo ululu tchimo wachotsedwa. Madalitso a Mulungu si a munthu aliyense. Ndi a anthu ake owerengeka. Madalitsowa ndi a akhristu okha basi. Kodi mukudziwa motsimikidzika mtima kuti ndinu wa Yesu?

Izi ndizomwe zingakuthandidzeni kudziwa kuti inu ndi nkhristu:

1. Vesi 9 ikunena kuti tiitanire padzina la Mulungu ndikumutumikira Iye "mogwirana manja" ndi akhristu a nzathu. Tikuyenera kumukhulupirira Iye ndi mtima wathu wonse, komanso kumutumikira mokhulupirika.

2. Vesi 11-12 akutiudza kuti tikuyenera kugonjetsa kuzikuza kwathu, ndikukhala ofatsa komanso wodekha. Uzichose wekha pa mpando ndikumutsiya Yesu kuti pamalo pako.

3. Akhristu Monga vesi 13 ikutiuzira, akuyenera kufunafuna kukhala moyo wa chiyero. Tikuyenera kuyetsetsa kunvera Mulungu. Yohane 14:15 akunena kuti ngati tikonda Mulungu tikuyenera kunvera Iye. Tidzakhala oyera pamene tikukulirakulira mukunvera.

Takuuzidwa tsopano pa vesi 14 kuimba Nyimbo yatsopano ndi chimwemwe. Vesi 15 ikutiuza kuti tikuyimba Nyimbo imeneyi chifukwa Mulungu wachotsa chilango chathu kotero wabwerera kwa ife.

Kuyambira apa mpaka kumapeto kwa buku la Zefaniya ndi uthenga wa chilmbikitso champhamvu. Vesi 17 ndiyokhayo yotonthodza. Apa Zefaniya akutiudza kuti Mulungu ali okondwa ndi anthu ake-akhristu-kotero kuti akuyimba pamodzi ndi ife mokondwera.

Hagai

Hagai ndi Zakariya anali aneneri anthu atabwerera kuchoka ku ukapolo. Amatchedwa kuti ndi aneneri pambuyo pa ukapolo chifukwa adagwira ntchito imeneyi pamene Ayuda anabwera kuchokera ku ukapolo. Onse adagwira ntchito nthawi imodzi, ndipo cholinga chawo ndikupangitsa Ayuda kuchilimika pomanganso kawiri kachisi ndikuti chipembezo chimbenso kuchitikira mmnenemo. Itatha nthawi yao ya ukapolo, Ayuda amafunikira kulimbikitsidwa, amafuna chitsitsimutso. Mulungu adatumidza aneneri amenewa pa zifukwa zimenezi.

Ayuda omwe Hagai amayankhula nawo anali otsiyana ndi Ayuda omwe analiko chionongeko chisanachitike. Anali ngati akhristu ambiri lero omwe ali ngati anthu a Mulungu, koma amalabadira za iwo eni kenako Mulungu. nthawi zambiri anthu a Mulungu amakhumba kutumikira Mulungu, koma amayamba adzitsamalira iwo eni, kenako ngati ali ndi nthawi, kapena ndalama yotsala ndipamene tsopano amakumbukira Mulungu.

Pamene anabwerera ku Yerusalemu koyamba anayamba kumanganso kachisi, koma posakhalitsa zolepheretsa ntchitoyi zidayamba ndipo ntchitoyi inayima. Panatatha zaka 50 nasagwira ntchito iliyonse yopitiridza kumanga kachisi. Kotero Mulungu anatumiza Hagai kuti alimbikitse anthu kupitiliza kumanga kachisi.

Hagai 1:2 akutiuza kuti anthu anaganiza kuti nthawiyo siinali yoyenera kuti amange kachisi. Chifukwa chimene Mulungu anawabwedzeretsera anthu ku Yerusalemu kunali kumanganso kachisi ndicholinga chakuti ayambenso kupembeza Mulungu moyenera. Anthu anayamba kunyozera nfundo imeneyi.

Vesi 3-11 yanena za yankho la Mulungu pa maganizo a anthu oti asamange kachisi. Mulungu anabweretsa uthenga wake kwa anthu kudzera mwa Hagai. Koyamb mu vesi 4 akuonetsa mau azuzula chifukwa anthu ayika patsogolo Nyumba zawo ndikuika pambuyo Nyumba ya Mulungu. akupitiriza kulongosola mu vesi 10-11 kuti njala yomwe ili pakati pawo ndichifukwa chakunyozera kwawo kumanganso Nyumba ya Mulungu. akufunikira kukhulupirira Mulungu ndikuchita ntchito yake asanayambe kuzisamalira iwo eni.

Tikuona mu vesi 12 kuti atsogoleri akunvera Mulungu ndipo pansi pa utsogoleri wao anavomera polonjeza kuti anvera Mulungu. Fananizana vesi 1 ndi 15, tikuona kuti kuyankha kwa anthu kunali kwa m’mangum’mangu. Kwa matsiku 23 okha anthu anayamba kugwira ntchito yomanganso kachisi.

Anthu mosatenga nthawi anakhumudwitsidwanso, monga tikuonera pa chaputala 2:1-9. Anakhumudwitsidwa chifukwa:

1. Ntchitoyo inali yakalavula gaga, ndipo koyamba, onse anayenera kuchita anayeneranso kuchotsa zinyalala pamalo pomwe panali kachisi wakale. Kachisi wakale anali ataonongeka kwanthunthu, ndipo inali ntchito yaikuru kwambiri kukonza malowa kuti ntchito yomanga kachisi kachiwiri iyambike. Panalibe chimaoneka kutsintha kufikira ntchito yopotsa itachitika.

2. Analibe zipangizo zokwanira kuti amange kachisi wankuru komanso wodemerera monga momwe analili wa poyamba uja. Hagai mu vesi 3 anauza anthuwo kuti kachisi yemwe amange kachiwirika adzakhala kachisi ocheperako kutsiyana ndi wapoyamba kachisi wa Solomo.

Mulungu mu vesi 4 akulimbikitsa anthu. Hagai anawauza kuti alimbike ndikupitilidza kugwira ntchito chifukwa Mulungu ali nawo limodzi. Uwunso unali uthenga womwe Mulungu anapereka kwa ogwira ntchito ake nthawi ya m’mbuyomo. Yoswa 1:6-9; 1 Mbiri

28:20. Ndi uthenga omwewu omwe Mulungu akupereka kwa ogwira ntchito ake lero. Izi ndi zina mwa zifukwa zomwe Mulungu amanenera kuti anthuwo alimbike;

1. Mu vesi 5 Mulungu akukumbutsa anthuwo za pangano lomwe anapanga ndi anthu ake pamene anawaturutsa mu Aigoputo ndikuwatsamalira. Anawakumbutsa kuti adzakhala nawo limodzi nthawi zonse.

2. Mulungu anawakumbutsa mu vesi 8 kuti iye ndiye mwini golide ndi siliva (Masalmo 24:1) ndipo adzawapatsa chilichonse chomwe ali kufuna.

3. Mulungu akulonjeza mu vesi 7 kuti adzabwera ndi kudzaza mu kachisiyo ndi ulemerero wake. Ulemerero wa kachisi watsopanoyu, akupezeka mwa Mulungu, osati mu kukula ndi chuma cha katundu wake. Nkhani si maonekedwa akunja, koma mtima ndiomwe umayang'anidwa kopotsa. Ulemerero wa Mulungu umapezeka mu mpingo womwe anthu ake ali ndi mitima yoyang'na pa Mulungu, kotero kuoneka bwino kapena kukula kwa tchalichi kulibe ntchito.

Uthenga wotsatira kuchokera kwa Mulungu unaperekedwa kupita kwa amsembe vesi 10-19. Hagai anafunsa mafunso awiri kwa ansembe omwe anawayankha:

1. Vesi 12 funso ndilakuti, chinthu choyera chikakhudza chinthu chodetsedwa kodi chodetsedwacho chimakhala choyera? Yankho la amsembe likuti ayi ndithu.

2. Vesi 13 funso, chinthu wamba chikakudza chinthu choyera kodi choyeracho chimadetsedwa? Yankho ndilakuti inde.

Tsopano kuti mau akakhadzikike, Hagai mu vesi 14 akunena kuti izi ndizomwe zachitika kwa anthu ndi ntchito zawo. Anthuwa akugwira ntchito pa kachisi, koma mitima yao ili kutali ndi ntchitoyi. Akungogwira ntchito chifukwa kunva kutero. Titumikire Mulungu ngati mtima wathu uli pa ntchutoyi, ndipo tisachite izi mokakamizika.

Mulungu akuitana anthu mu vesi 15-17 kukumbukira zolephera zawo zam'mbuyo zomwe zinachitika chifukwa cha khalidwe la mitima yao. Tsopano pa vesi 18-19 Mulungu akuitana anthu kukhala ndi khalidwe latsopano pobwera kwa Mulungu. ndipo akulonjeza kudalitsa anthuwo.

Uthenga wosiliza ukupezeka mu vesi 20-23 ndipo ukulunjika kwa Zerubabelo yemwe anali gavanala. Dziko linali losakhadzikika nthawi imeneyi. Yuda anali wang'ono kwambiri koma anazungulilidwa ndi maiko oyipa kwambiri. Anthu amakaikira za chitetezo chawo. Uthenga wa Mulungu mu vesi 21-22 ndiwakuti Iye ali kulamulira chilichonse kotero anthu asachite mantha. Uthenga umenewu ukukhudzanso ife lero.

Zekariya

Zakariya ndi limodzi mwa buku lovuta kulinvetsetsa mu Chipangano Chakale. Tikudziwa kuchokera mu vesi 1 kuti uthenga wake unabwera pamene Ayuda anabwera ku Yerusalemu kuchokera ku ukapolo. Anali ndi anthu oyamba kubwerera kuchokera ku ukapolo pansi pa utsogoleri wa Zerubabelo ndipo ananenera panthawi yomwe Hagai anali kuneneranso. Uthenga wake unali olimbikitsa Ayuda amene alangidwa ndi Mulungu ndipo pano akukumana ndi nyengo zovuta zomanganso kachisi ku Yerusalemu.

Uthenga wa Zakariya kwa Ayuda unali wakuti ngakhale zinthu zinali zovuta kwa iwo, koma panali tsogolo laulemerero lomwe limawayembekezera. Ulosi wake umanena zonse, kubwera koyamba ndi kachiwiri kwa Mesiya.

I. Mbali yoyamba ya bukuli, ikupezeka pa chaputala cha 1:1-6 ndipo ndikuitana anthu kuti alape. Zakaliya akukumbutsa anthu kuti asakhale osanvera ngati makolo awo omwe

anapangitsa Mulungu kuti awapatse chilango. Mulungu akulonjeza anthuwo kuti akabwerera kwa Iye, kotero azachotsa mkwiyo wake pa iwo monga anachitira ndi makolo awo oyamba. Ngati anthu alapa ni kunvera Mulungu, adzawalandira iwo. Uwu ndi uthenga kwa mipingo lero lino, kuti ngati anthu alapa ndikutembenukira kwa Iye-Mulungu adzawalandira iwo.

II. Zakariya, mu chaputala 1:7-6:8 akulandira masomphenya asanu ndi atatu kuchokera kwa Mulungu, omwe anaperekedwa usiku umodzi. Mwachidule masomphenyawo ndi awa:

1. Masomphenya oyamba ali mu chaputala 1:7-17. Mngelo wa Mulungu ooneka ngati munthu anali pa kavalo. Munthuyu amanena kuti dzikoli likhala la bata. Izi zikutsokoneza Mulungu chifukwa Yerusalemu ndi Yuda akuvutika ndipo alibe mtendere. Mu vesi 16-17 Mulungu akulimbikitsa anthu ake mu Yerusalemu ndi Yuda pakuwalonjeza kuti adzawadalitsa ndi ochumantsogolomo.

2. Tikupeza nyanga zinayi mu 1:18-19 mu masomphenya achiwiri. Nyangazi zikuimira maiko anayi kuchokera mu Danieli 7:1-8.

3. Masomphenya achitatu akuonetsa munthu akuyetsa Yerusalemu.

4. Masomphenya achinayi, akuyamba mu 3:1, akuonetsa nkuru wansembe, Yoswa atavala zovala zosalongosoka, zomwe zikuimirira machimo a Yoswa, ndi anthu. Satana ndiye ososa Yoswa, ndipo Mulungu akunena kuti adzachotsa tchimo la Yoswa. Uwu ndi ulosi wa Mesiya. Chaputala 3:9 akunenera za kuchotsedwa kwa tchimo la dzikolo mutsiku limodzi zomwe zikulosera za chotetedzera. Chotetedzera apa, chikuimirira kubwera kwa nsembe ya Yesu pamene anapachikidwa pamtanda ndipo Mulungu atate anavomereza chilango chimenechi, ngati dipo la machimo a akhristu onse. Izi zikutanthaudza kuti ife akhristu tili pa chiyanjano ndi Mulungu.

5. Ulosi wa chisanu, ukupezeka pa mutu 4 ukunena za choikapo nyali cha golide, ndi mitengo iwiri ya azitona. Choikapo cha golide chikuimirira kuti anthu a Mulungu ndi kuunika kwa dziko lapansi. Yesu ananena zokhudzana ndi izi pa Mateyu 5:14. Mitengo ya azitona ikuimirira okhala m''maudindo, mafumu ndi amsembe a ku Israyeli, amene anali Zerubabelo ndi Yoswa pamene ulosiwu umalembedwa. Kenako Yesu anabwera ngati wansembe komanso Mfumu.

6. Masomphenya achisanu ndi chimodzi akupezeka mu chaputala 5:1-4 pamene Zakariya anaona buku lowuluka (mpukutu wa mapepala olembalamba). Uthenga womwe unalembedwa pa mapepalawo ndiokhudzana ndi machimo akuba ndi onama. Izi zingakuzedwa kuphatikidzapochiweruzo kapena chilango cha machimo onse.

7. Mkazi ndi efa akupezeka m'masomphenya achisanu ndi chiwiri, mu chaputala 5:5-11. Mkaziyu akuimira choipa chomwe chichotsedwe kwa ana a Israyeli, ndikupititsidwa ku Sinara, komwe tikukumbukirako kuchokera mu Genesis 11:2, kuti anali malo komwe anthu anakaukira Mulungu ndikumanga msanja ya Babele. Izi zikuimirira kuchotsa kwa tchimo mu Israyeli; kuchotsa ngakhale maganizo a uchimo.

8. Masomphenya osiliza akupezeka pa mut 6:1-8 amene akuonetsa magaleta anayi amene akuyenda padziko lonse lapansi kubweretsa chiweruzo cha Yehovaku dziko lonse.

III. Lamulo loveka Yoswa korona 6:9-15. Lamulo laperekedwa loveka Yoswa nkuru wansembe kolona. Izi zikuyang'ana kubwera kwa Mesiya chifukwa palibe munthu amene amaloledwa kukhala mfumu komanso wansembe nthawi imodzi. Mesiya adzakhala ndi maudindo onsewa, mfumu komanso wamsembe.

IV. Funso la kuyenjezera masiku a kusala kudya 7:1-8:23. Chipangano Chakale chimalamulira kuti pazikhala tsiku limodzi lakutsala kudya kwa chaka chonse lomwe linali

tsiku la chotetedzera. Kuchokera pamene Yerusalemu anagwa, Ayuda anakhala akusala kwanthawi yochulukirapo pachaka pokumbukira kugwa kwa mzinda wawo. Tsopano anthu abwedzeretsedwa ku Yerusalemu, koma tsopano funso lawo nkumati, nanga nkupitilizabe kusala kudya kumeneku. Yankho la Mulungu ku funso limeneli linali lakuti, iye amakondwera kwambiri ndi kunvera kupotsa kusala kudya. Mulungu amakondwera ndi makhalidwe a mumtima a munthu kutsiyana ndi zimene amachita kunja kuti azionetsere kwa anthu, zinthu monga ngati kusala kudya. Mulungu akulonjeza madalitso kwa anthu ake ngati angalemekeze Mulungu munjira yomwe akukhalira.

V. Mutu 9-10 ndi masomphenya atsopano.

1. Chaputala 9:1-8 akunena za kubwera kwa mgonjesi (Alekizanda wankuruyo) amene anagonjetsa maiko onse omwe anazungulira Israyelimalinga ndi ndondomeko yomwe ikunenedwa mu bukuli. Masomphenyawa akunena kuti Alekizanda sadzaononga Yerusalemu, ndipo zoonadi sadaononge Yerusalemu.

2. Tikupeza chithunzi cha Mesiya mu vesi 9-10. Vesi 9 ikuonetsa mfumu Yesu akulowa mu Yerusalemu (onani Mateyu 21:5).

3. Mutu 9:14-17 kachiwiri akunena za kubwera kwa Mesiya amene akudzakhala mfumu; mfumu yomwe imatetedza anthu ake monga amachitira Mbusa ndi nkhosa zake. Izi ndizotsiyana ndi mafumu ena amene amagwiritsa ntchito anthu kuti angokhutitsa mimba zawo.

VI. Mutu 11 ndiovuta kuunvetsetsa, koma titha kunena kuti ukulosera chilango choopsa kwambiri. Ena amaganiza kuti mutuwu umatanthaudza kubwera kwa chionongeko cha Yerusamu kuchokera kwa Aroma mu chaka cha 70 AD.

VII. Mutu 12-14 uli ndi masomphenya a tsopano.

1. Mutu 12 ukunena momwe Yerusalemu adzachitiridwe chiwembu, ngakhale adani akuyetsa ngati atha kugonjesa Yerusalemu mophweka, Mulungu adzaonetsesa kuti chiwembu chawo chisapindule. Chimodzimodzi ndi mpingo wake lero. Pali ziwembu zambiri zomwe mpingo ukukumana nazo. Koma Mulungu adzateteza mpingo kotero kuti sudzaonongedwa padzakhala ena otsala.

2. Mutu 13 ukuyamba mu vesi 1 kunena kuti anthu adzasukidwa machimo awo. Vesi 7-9 ikunena za imfa ya Mbusa Wabwino (Yesu). Pambuyo pa izi, omusatira ake azamwazika ndipo adzakumana ndi mayetsero adzaoneni, ndipo pamene adzayengedwe adzabweretsedwa pamaso pa Mulungu. Anthu a Mulungu adzaitana padzina la Mulungu ndipo Mulungu adzawalandira iwo ngati anthu ake.

3. Mutu 14 ikutseka bukuli pakuyang'ana kutsogolo. Iyi ndi ndime yovuta kuinvetsetsa, koma zikuoneka kuti ikuyang'ana kutsogolo pamene Israyeli adzakhale kawiri dziko. Kenako maiko ena adzafuna kuchitira chiwembu, Israyeli, koma Mulungu adzalowererapo vesi 3, ndipo adaniwo adzagonjetsedwa.

A. Vesi 6-11 akunena kuti Mulungu adzakhala ndi anthu ake, ndipo kudzakhala dalitso lalikuru ndi a Israyeli pamene adani awo adzakhale atagonjetsedwa.

B. Gawo lotsatira lili ndi mavesi 12-15, limene likunena kuti padzakhala chilango/chiweruzo chachukuru kwa adani onse a Mulungu. vesi 16-19 akunena kuti maiko onse omwe adzatembenuke ndi kutsata Mulungu adzadalitsidwa.

4. Mavesi awiri akumapeto, akunena kuti tsiku likubwera pamene chilichonse chidzakhale choyera. Kumwamba kudzakhala koyera; kumwambako sikudzakhala tchimo.

Malaki

Malaki akutseka Chipangano Chakale ndi kuyang'ana ku Chipangano Chatsopano. Bukuli linalembedwa m'masiku a Nehemiya. Mneneri Malaki anabweretsa uthenga wa chikondi ndi machebjezo kwa anthu a Mulungu. bukuli linalembedwa ngati zokambirana pakati pa Mulungu ndi anthu ake. Mwa mavesi 50 mavesi 47 ndi zonena za Mulungu.

1. Mulungu akuyamba mu chaputala 1:5 kuudza anthu kuti amawakonda, ndipo chitsimikidzo cha chikondi chake chikuoneka pamene anagonjetsa m'dani wawo; Edomu.

2. Kenako, mu 1:6-2:17 Mulungu akunena kuti anthu akupitiridza kunyozera chikondi cha Mulungupakusamulemekedza ndi kumvera Iye.

A. Vesi 6-8 Mulungu akuzuzula anthu chifukwa chakusamulemekedza ndi nsembe zawo zosalemekezeka.

B. Mu chaputala 2:5-9 Mulungu akudandaula kuti ansembe ake sakuphunzitsa choonadi chokhudzana ndi Iye, kwa anthu. Mulungu amafuna Baibulo kuphunzitsidwa mokhulupirika, liphunzitsidwe kwa anthu onse, okalamba ngakhale achinyamata, mkazi komanso mwamuna. Akuru a mpingo ali ndi udindo pa kuphunzitsa kumeneku.

C. Chaputala 2:11 Mulungu kachiwiri akuzuzula anthu ake pokwatira akazi a chilendo. Pamene tikufika kumapeto kwa Chipangano Chatsopano, tikuona kuti anthu sanalapebe.

D. Dandaulo lotsatira la Mulungu, mu vesi 14-16 ndilakuti anthuwo amatsiya akazi awo.

E. Vesi 10 muli dandaulo lakuti anthu sakondana wina ndi nzache. 1 Yohane 4:7-12 akutiudza kuti ife akhristu tikuyenera kukondana wina ndi nzache ngati sititero ndiye kuti si ife akhristu.

F. Tikuona mu vesi 17 kuti anthu akunena kuti Mulungu amakondwera muchikhalidwe chawo chachabe, lomwe lili bodza la nkunkhuniza. Mulungu sakondwera mu machimo a anthu ake.

G. Mulungu akunena kuti posayang'anira kulephera kwa anthuwo, Mulungu adzaonetsa kwa iwo dzina lake labwino.

3. Mutu 3:1-6 ukunena za kutsogolo maka poyang'ana kwa Yesu.

A. Vesi 1 akulotsera za kubwera kwa Yohane M'batizi amene adzalengeze kubwera kwa chiweruzo chabwino. Uyu ndi Mesiya.

B. Vesi 2-4 akunena kuti Mulungu wa chiweruzo azabweretsa chiweruzo osati kwa maiko a mitundu okha komanso kwa Ayuda eni ake.

C. Tikudziwitsidwa mu vesi 6 chimodzi mwa nkhalidwe la Mulungu. Mulungu wathu sasintha. Ndioyera zomwe zikutanthaudza kuti Iye ndi wangwiro ndipo adzakhala chomwechi mpaka kalekale. Lonjezo lililonse lomwe Mulungu amapanga ndiloona lero monga momwe linalili pamene amachita lonjezo limeli chifukwa palibe chomwe chimasintha ndi Mulungu.

4. Malaki 3:7-12 akunena momwe Mulungu anazuzulira anthu pomumana chakhumi. Mulungu akuwonetsa poyera kuti tikuyenera kumpatsa ndalama zathu ndipo ichi ndichimodzi mwa kukhulupirira Mulungu.

5. Malaki 3:13-18 tikuona kuti anthu ambiri alibe chidwi ndi zinthu za Mulungu monga momwe ziyenera kukhalira. Tikuona mu vesi 16-17 kuti ngakhale mudziko limeneli lomwe ambiri mwa iwo ndi osakhulupirira koma Mulungu alimo ndi anthu ake okhulupirika. Dziko lero lili chimodzimodzi ndi zomwe tikuziona apazi, ngakhale mumpingo wake, anthu ambiri sanvera Mulungu, komabe ali ndi anthu ake ochepa omwe ali akhulupirika.

6. Mutu 4:1-3 muli machenjezo osiliza kwa anthu osanvera.

7. Chaputala 4:4 Mulungu akuseka Chipangano Chakale ndi kukumbutsa anthu kunvera Malamulo ake monga kunapasidwa kwa Mose. Mu vesi 5-6 Malaki akutseka polonjeza kuti Mulungu adzatumidza wina wake yemwe adzabweretse anthu ku kulapa. Kugwiritsa ntchito dzina la Eliya apa kumasokoneza kwambiri ndipo kwabweretsa kusagwirizana kwambiri. Sizikudziwika bwinobwino kuti Eliya akunena za ndani.